

UKADAULO

WA

KASANTHULIDWE KA BAIBULO

HARVESTIME INTERNATIONAL INSTITUTE

Phunziro limeneri ndi gawo limodzi la maphunziro a **Harvest International Institute** ndipo cholinga chake ndi kukonzekeretsa okhulupilira kuti akatute zokolora zambiri zauzimu.

Mutu waukulu mumaphunzirowa ndikuphunzitsa zimene Yesu anaphunzitsa, zimene zinasandulitsa anthu wamba monga asodzi, otolera misonkho ndi ena kulalikira Uthenga Wabwino ndi kuwonetsera mphamvu ya uthengawo mu nthawi yawo.

Bukuli ndi phunziro limodzi mwa maphunziro ambiri amene cholinga chake ndikuwakopa okhulupilira kuti akakonze dongosolo, kuyendetsa, ndi kubweretsa pamodzi anthu kuti Uthenga Wabwino ukalalikidwe.

ZAMKATI MWA BUKULI

| | |
|--|---|
| Kagwiritsidwe ntchito Ka bukuli..... | 3 |
| Ndondomeko Zothandizira Kuphunzira limodzi Pagulu..... | 4 |
| Mau oyamba..... | 5 |
| Zolinga za Maphunzirowa..... | 7 |

GAWO 1: MUTU WA PHUNZIRO

| | |
|--------------------------|----|
| 1. Kudziwa Baibulo..... | 8 |
| 2. Mabuku a Baibulo..... | 22 |

GAWO 2: KUKONZEKERA KUSANTHULA

| | |
|---|----|
| 3. Musanayambe..... | 44 |
| 4. Mfundo zakatanthauziridwe ka Baibulo..... | 54 |
| 5. Mbiri Ya Baibulo..... | 62 |
| 6. Kusanja mitu, kuiza zizindikiro ndi kugawa nkhani..... | 76 |

GAWO 3: KUSANTHULA BAIBULO MWALUSO

| | |
|---|-----|
| 7. Kusanthula Baibulo ndi Baibulo..... | 82 |
| 8. Kusanthula Mau Momangilira moyo Wauzimu..... | 96 |
| 9. Kusanthula Buku..... | 108 |
| 10. Kusanthula Chaputala..... | 116 |
| 11. Kusanthula ndime..... | 129 |
| 12. Kusanthula vesi..... | 139 |
| 13. Kusanthula Liu..... | 145 |
| 14. Kusanthula Baibulo potsata Mutu..... | 156 |
| 15. Kusanthula Baibulo poyang'anira Moyo wa Munthu..... | 163 |
| 16. Njira yosanthula Chiphunzitso..... | 173 |
| 17. Kusanthula mabuku a ndakaturu..... | 189 |
| 18. Kusanthula ma Buku a ulosi..... | 199 |
| 19. Njira ya chifaniziro..... | 219 |
| Njira zina zosanthulira Baibulo..... | 230 |
| Mayankho amafunso odziyesa nokha..... | 233 |

KAGWIRITSIDWE NTHCITO KA BUKULI

KAKONZEDWE KA BUKULI

Phunziro liri lonse limakhala ndi zinthu izi:

Zolinga: Izi ndi zimene mukuyenera kukwaniritsa kapena kudziwa pa mapeto pa phunziro. Welengani zimenezi musanayambe phunziro lanu.

Vesi Yotsogololera: Ndimeyi imatsindika mfundo yayikulu mu phunziro lathu.

Zopezeka mu Magawo: Gwiritsani ntchito Baibulo lanu kuti mufufuze mavesi amene sanalembedwe mu bukuli koma angotchulidwa.

Mayeso Odziyesa Nokha: Osathamangira kulemamba mayeso musanamalize kuwerenga chaputala, komanso polemba musagwiritse ntchito Baibulo kapena bukuli polemba mayesowa. Mayankho amayesowa muwapeza kumapeto a bukuli.

Zophunzira Zowonjezera: Ndime imeneyi ikuthandizani kuti muwerenge mau Mulungu ndi kuzamitsa ukadaulo wanu pophunziro komanso kugwiritsa ntchito mu utumiki zimene mwa.

Mayeso Omaliza: Ngati mwayamba kuphunzira phunziroli mukuyenera kulemba mayeso pamapeto a phunziroli ndipo mayesowo aperekedwa kwa aphunzitsi anu kuti mupatsidwe malikisi.

ZOWELENGA ZINA ZOFUNIKA POHUNZIRA PHUNZIROLI

Mudzafunikira Buku Lopatulika

NDONDOMEKO ZOTHANDIZIRA KUPHUNZIRA LIMODZI PAGULU

MKUMANO WOYAMBA

Kutsekulira: Yambani ndi pemphero ndi kudziwana wina ndi mnzake ndipo ophunzira alembetse mayina.

Khazikitsani Ndongomeko Zapagulu: Musankhe amene atsogolere mkumano wanu, sankhaninso malo ndi masiku amene muzikumana.

Mayamiko ndi Matamando: Yitanirani kupezeka kwa Mzimu Woyera pamene muchita mkumano wanu.

Gawani Mabuku Kwa Ophunzira: Awuzeni ophunzira dzina laphunziro, zolinga zake ndi dongosolo.

Perekani Ntchito Yoyamba. Ophunzira ayenera kuwerenga ma chaputala amene apatsidwa ndikulemba mayeso odziyesa okha isanafike nthawi ya mkumano wina. Ndipo kuchuluka kwa machaputala amene aziphunzitsidwa pa mkumano uli wonse kuzitengera kutalika kwa chaputala komanso kumvetsetsa kwa ophunzira.

MKUMANO WACHIWIRI NDI KUKUMANA KWINA PATSOGOLO

Kutsekulira: Tsekulirani ndi pemphero kenako lembani mayina a ophunzira atsopano ndikuwapatsa buku lawo. Muyitane mayina a ophunzira amene abwera. Komanso osayiwala mayamiko ndi matamando kwa Mulungu.

Kukumbutsira: Yambani ndi kubwereza mwachidule zimene munaphunzitsa mu mkumano wanu womaliza.

Phunziro: Afunseni ophunzira ndemanga zawo kapena mafunso okhudza phunziro limene aphanzira komanso m'mene angagwiritsire ntchito zimene aphanzira pamoyo wawo ndi utumiki.

Mayeso Odziyesa Nokha: Konzetsani mayeso amene ophunzira amaliza ndipo mukhonza kusankha kupereka mayankho kapena kuwachotsa mubukuli kuti ophunzira adzipezere okha mayankho.

Mayeso omaliza: Pamapeto pa maphunziro amenewa, gulu la ophunzira onse lidzapemphedwa kulemba mayeso omaliza ndipo aphanzitsi awonetsetse kuti ophunzira wina aliyense ali ndi buku laphunziroli.

MAU OYAMBA

Mneneri wa m'Chipangano Chatsopano amadziwika ngati “mau ofuula m'chipululu’ pamene amalalikira Mau a Mulungu. Uthenga wake unali watsopano, wamphamvu komanso wolingana ndi zosowa zauzimu za anthu a nthawi yake.

Anthu ambiri lero akumva mau a choonadi omwe akumveka m'lengalenga pafupi nawo. Iwowo siliu lomwe Mulungu akugwiritsa ntchito kubvumbulutsa uthenga wake, iwowo ndi liu longomveka kuchokera kwa ena. Ali ngati aneneri omwe Mulungu ananena kuti, “amene amaba mau anga, yense kum'bera mnasi wake” (Yeremiya 23:30).

Kuti mulankhule Mau a Mulungu, mukuyenera kudziwa chomwe Mulungu walankhula. Cholinga cha phunziro lino ndicho kukukonzekeretsani kuti mukathe kumvetsa bwino Mau a Mulungu. Mudzafunika bukhu lino, Baibulo lanu, ndi chitsogozo cha Mzimu Woyera basi kuti muphunzire “Njira Zaluso Posanthula Mau” zimenezi.

Njira ndi dongosolo lapadera lochitira zinthu. Njira zosanthulira Mau madongosolo omwe amaikidwa othandizira kusanthula bwino Mau olembedwa. Mau akuti “mwaluso” amatanthauza “kutekera kopanga kanthu kena katsopano.” Phunziro lino likuphunzitsani kusanthula Mau a Mulungu panokha. Simukuyenera kudalira kafukufuku wa anthu ena chifukwa muzikwanitsa kusanthula Mau a Mulungu panokha ndikupanga madongosolo osanthulira Mau.

Pakuphunzira njira zosanthulira mau zoyenera mudzakhala liu limene Mulungu adzagwiritsa ntchito kubvumbulutsa choonadi ku dziko lokhala ndi njala yauzimu. Simukhalanso mau chabe omveka kuchokera kwa anthu ena.

“Njira za Kasanthulidwe Kaluso ka Baibulo” ndi phunziro lomwe lizindikira kuti Baibulo ndi mau a Mulungu m'modzi wona. Limafotokozerana momwe Baibulo lidagawidwira komanso matanthauziridwe osiyana-siyana. Poyamba phunziroli likutsogolerani pakuzindikira zomwe Baibulo limaphunzitsa, kenako nkufotokozerana njira zaluso za kasanthulidwe ka Baibulo ndi kukupatsani mwayi woti mugwiritse ntchito njira iriyonse yomwe yaperekedwa.

Phunziro lino limaonanso momwe mungakonzere mlozo, kulemba zomwe mwaphunzira, komanso kuika chizindikiro pandime za m'Baibulo, ndi kupanga ndime zazitali kukhala zowerengeka mosavuta. Phunziroli likuthandizanso pa katanthauziridwe ndi kagwiritsidwe ntchito ka Mau a Mulungu moyenera. Ndipo likupangani maso anu kuyang'ana pa Mphunzitsi

Wamkulu, Mzimu Woyera. Ngati mutsatira ndondomeko zimene ziperekedwe m'bukhu lino, muona kusintha kwakukuru pamoyo wanu wauzimu.

Palibe njira ya kasanthulidwe ka Baibulo yomwe ingatenge malo a utumiki wa kuphunzitsa wa Mzimu Woyera. Iye ndi mphamvu yauzimu yomwe imapangitsa njirayo kukhala yaluso ndi yopindulitsa. Amanong'oneza mu mzimu wa munthu choonadi cha Mau a Mulungu zomwe zimabweretsa moyo watsopano wauzimu kuti uyende pa munthuyo.

Kuphunzitsa njira za kasanthulidwe sindiye cholinga chathu chachikuru. Koma kuti zingotithandizira kuti tikakwaniritse cholinga chathu chachikuru ndicho kusanthula Mau a Mulungu. Kuphunzira njirazi sikokwanira. Mukuyenera kugwiritsa ntchito zomwe mwaphunzira pa kusanthula Mau a Mulungu ndi kugwiritsa ntchito choonadi chake pa moyo ndi utumiki wanu.

Ngakhale mumaliza maphunziro onse omwe ali m'bukhu lino, koma chilungamo chake nchakuti phunziro lino simungalimalize. Kasanthulidwe kanu ka Mau a Mulungu sikadzatha pakuti palibe amene anganene kuti ine ndamaliza kuphunzira zinsinsi zonse zauzimu.

ZOLINGA ZA MAPHUNZIRO ANO

Pamene mumaliza maphunziro a m'bukhu lino, mukhala mukukwanitsa:

- Kufotokoza m'mene Baibulo linapezekera
- Kufotokoza dongosolo la magawidwe a Baibulo m'zipangano, magawo akuluakulu ndi mabuku.
- Kufotokoza mwachidule mbiri ya mndandanda wa zochitika m'Baibulo.
- Kufotokoza kugwirizana ndi kusiyana kwa kalembedwe ka Baibulo
- Kufotokoza momwe kabweredwe ka matanthauziridwe osiyanasiyana a Baibulo.
- Kugwiritsa ntchito malamulo a katanthauziridwe koyenera ka Baibulo
- Kulemba mwachidule zomwe Baibulo limaphunzitsa zokhuza ilolo.
- Kudziwa zomwe zimafunika pa kasanthulidwe ka Mau a Mulungu.
- Kukonza milozo, zojambula, kudula mzere kungsi kwa ndime komanso kulemba zomwe mwaphunzira mwachidule kuti muzitha kukumbukira zomwe mwaphunzira mosavuta.
- Kugwiritsa ntchito njira zaluso pamene musanthula Mau a Mulungu
- Kugwiritsa ntchito zipangizo za kasanthulidwe ka Baibulo.

GAWO 1: MUTU WA PHUNZIRO

CHAPUTALA 1

KUDZIWA BAIBULO

ZOLINGA

Mukamaliza chaputala chino muzikwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kupereka tanthauzo la mau oti “Baibulo.”
- Kupereka tanthauzo la mau oti “Malemba.”
- Kufotokoza komwe kudachokera Baibulo
- Kudziwa zolinga zikuluzikulu za Baibulo
- Kudziwa Chipangano Chakale ndi Chatsopano ngati magawo akuluakulu a Baibulo.
- Kutchula magawo anayi a mabuku a m’Chipangano Chakale
- Kutchula magawo anayi a mabuku a m’Chipangano Chatsopano
- Kufotokoza tanthauzo la “kugwirizana ndi kusiyana” kwa Baibulo
- Kudziwa munthu amene ndiye pokhazikika pa mabvumbulutso a m’zipangano zonse.

VESI LOTSOGOLERA

Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa ciphunzitso, citsutsano, cikonzero, cilangizo ca m'cilungamo: kuti munthu wa Mulungu akhale woyenera, wokonzeka kucita nchito iri yonse yabwino. (2 Timoteo 3:16-17)

MAU OYAMBA

Chaputala chino chikutipanga kukadziwa Baibulo monga Mau olembedwa a Mulungu m’modzi ndi woona. Mau oti “Baibulo” amatanthauza “mabuku.” Baibulo ndi bukhu limodzi lomwe lapangidwa ndi mabuku okwanira 66.

Mau oti “Malemba” amakhala akukambanso za Mau a Mulungu. Zolembedwa mouziridwa ndi Mulungu m’modzi ndi woona. Mau oti “Baibulo” sanagwiritsidwe ntchito m’Baibulo. Ndi mau omwe amagwiritsidwa ntchito ngati mutu wa Mau onse a Mulungu.

CHIYAMBI CHA BAIBULO

Baibulo ndi mau olembedwa a Mulungu. Iye anauzira mauwa ndipo anagwiritsa ntchito anthu okwana 40 kuti alembe mauwa. Ndipo ntchito yolembayi inachitika kwa zaka zokwana 1500. Chinthu chimodzi chachikulu chomwe chimagwirizanitsa anthuwa ndi umboni wakuti onsewa anatsogozedwa ndi Mlembi Wankulu m’modzi. Mlembi ameneyu ndiye Mulungu.

Ena mwa olembawa analemba zenizeni zimene Mulungu analankhula:

Tenga buku lampukutu, nulembe m'menemo mau onse ndanena kwa iwe akunenera Israyeli, ndi akunenera Yuda, ndi akunenera amitundu onse, kuyambira tsiku ndinanena kwa iwe, kuyambira masiku a Yosiya, mpaka lero. (Yeremiya 36:2).

Koma ena analemba zomwe zinawaonekera m’ moyo wao kapena zomwe Mulungu anawabvumbulutsira zokhuza tsogolo.

Ine Yohane, mbale wanu ndi woyanjana nanu m'cisautso ndi ufumu ndi cipiriro zokhala m'Yesu, ndinakhala pa cisumbu cochedwa Patmo, cifukwa ca mao a Mulungu ndi umboni wa Yesu. (Chibvumbulutso 1:19)

Olemba onsewa analemba mouziridwa ndi Iye mwini Mulungu mau a uthenga wake kwa ife.

CHOLINGA CHA BAIBULO

Baibulo limafotokoza lokha za cholinga chake:

Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa ciphunzitsa, citsutsano, cikonzero, cilangizo ca m'cilungamo: kuti munthu wa Mulungu akhale woyenera, wokonzeka kucita nchito iri yonse yabwino. (2 Timoteo 3:16-17)

Malemba akuyenera kugwiritsidwa ntchito pa kuphunzitsa chiphunzitsa, chidzudzulo, ndi kukonza cholakwika, ndi kuphunzitsa chilungamo. Adzakuthandizani kukhala moyo woyenera ndi kukukonzekeretsani ku ntchito ya utumiki.

MAGAWO AKULUAKULU A BAIBULO

Baibulo lagawidwa m'magawo awiri akuluakulu otchedwa Chipangano Chakale ndi Chipangano Chatsopano. Mau oti chipangano amatanthauza m'gwirizano. M'Chipangano Chakale muli dongosolo la pangano kapena mgwirizano woyamba wa Mulungu ndi anthu. Chipangano Chatsopano chinalembe za pangano latsopano la Mulungu kudzera mwa Mwana Wake, Yesu Khristu.

Kodi nkhani yaikulu m'mapangano awiri onsewa ndi yotani? Onsewa amakhuzana ndi kubwezeretsedwa kwa munthu wochimwa kuti akhale pa ubale wabwino ndi Mulungu. Mulungu anapanga lamulo lakuti tchimo lingathe kukhululukidwa pamene mwanzi wakhetsedwa:

Ndipo monga mwa cilamulo zitsala zinthu pang'ono zosayeretsedwa ndi mwazi, ndipo 2 wopanda kukhetsa mwazi kulibe kumasuka. (Ahebri 9:22).

Mu m'gwirizano wa Mulungu m'Chipangano Chakale, anthu amapereka nsembe za mwazi wa nyama kuti machimo awo akhululukidwe. Ichi chinali chizindikiro cha nsembe ya mwanzi yomwe Yesu adzapereke mu m'gwirizano watsopano ndi Mulungu. Kudzera m'kubadwa, moyo, imfa, ndi kuuka kwa Yesu, nsembe yomaliza inaperekedwa:

Buku Lopatulika 1992 Ahebri 9:11-15 Koma atafika Kristu, Mkuluwansembe wa zokoma zirinkudza, mwa cihema cacikuru ndi cangwiro coposa, cosamangika ndi manja, **ndiko kunena kuti, cosati ca ciengedweici, kapena mwa mwazi wa mbuzi ndi ana a ng'ombe, koma mwa mwazi wa iye yekha, analowa kamodzi ku malo opatulika, atalandirapo ciombolo cosatha. Pakuti ngati mwazi wa mbuzi ndi ng'ombe zamphongo, ndi makala a ng'ombe yamthandi owazawaza pa iwo odetsedwa, upatutsa kufikira ciyeretso ca thupi; koposa kotani nanga mwazi wa Kristu amene anadzipereka yekha wopanda cirema kwa Mulungu mwa Mzimu wosatha, udzayeretsa cikumbu mtima canu kucisiyanitsa ndi nchito zakufa, kukatumikira Mulungu wamoyo? Ndipo mwa ici ali Nkhoswe ya cipangano catsopano, kotero kuti, popeza kudacitika imfa yakuombola zolakwa za pa cipangano coyamba, oitanidwawo akalandire lonjezano la zolowa zosatha. (Ahebri 9:11-15).**

Zipangano zonse ziwiri ndi Mau a Mulungu ndipo tikuyenera kumaziwerenga limodzi kuti tikamvetse bwino uthenga wa Mulungu. Mau oti “chakale” ndi “chatsopano” akugwiritsidwa ntchito pongofuna kusiyantsa mapangano awiri amene Mulungu anapangana ndi munthu. Lina

Yesu asanabwere padziko kudzafa, lina atabwera. Sitikuyenera kunyoza Chipangano Chakale basi chifukwa chakuti chimatchedwa “chakale” ayi.

MAGAWO ENA A M’BAIBULO

Baibulo lagawidwanso m’ mabuku okwanira 66. Chipangano Chakale chiri ndi mabuku 39 ndipo Chipangano Chatsopano chiri ndi mabuku 27. Bukhu liri lonse lagawidwa m’mitu (chaputala) ndi ndime (vesi). Ngakhale kuti zomwe ziri m’ mabukuwa ndi Mau a Mulungu, machaputala ndi mavesi anaikidwabe ndi anthu ndi cholinga chakuti tisamavutike kupeza ndime yomwe tikufuna. Zikanamakhala zovuta kwambiri kupeza ndime achikhala kuti Baibulo liribe machaputala ndi mavesi.

Mabukuwa agawidwa motere:

BAIBULO

>

>

>

Chipangano Chakale

Chipangano Chakale

Mabuku 39

Mabuku27

KUGWIRIZANA KWA BAIBULO

Tikakamba za kugwirizana kwa Baibulo, timatanthauza zinthu ziwiri:

1. BAIBULO LIMAONETSERA UMODZI MU ZOLEMBEDWA

Ngakhale kuti Baibulo linalembedwa ndi anthu ambiri komanso kwa nthawi yaitali, liribe zinthu zotsutsana. Palibe wolembe wina yemwe analemba zotsutsana ndi zolembe za enawo. Mu Baibulo mumapezeka nkhani zovuta zambiri, nkhani zomwe zikatchulidwa anthu amakhala ndi kumvetsa kosiyanasiyana. Olemba Baibulo analemba nkhani zimenezi bwino lomwe ndi kugwirizana kwakukuru kuchokera Genesisi mpakana Chibvumbulutso. Izi zinali zotheka

chotere chifukwa wolemba anali m’modzi: Mulungu. Olembawo amalemba pansi pa chitsogozo ndi kudzodza kwa Mulungu. Chifukwa cha ichi zomwe timapeza m’Baibulo ndi zogwirizana.

2. BAIBULO LIMAONETSERA UMODZI PA MUTU WAKE

Anthu ena amaganiza kuti Baibulo muli mabuku 66 omwe akukamba nkhani zosiyanasiyana. Sazindikira kuti Baibulo ndilogwirizana popeza liri ndi mutu waukuru umodzi. Kuchokera ku mayambiliro kufikira kumapeto, Baibulo limabvumbulutsa cholinga chapadera cha Mulungu chomwe chalembedwa mwachidule m’bukhu la Aefeso:

Mwakonda cilungamo, ndi kudana naco coipa; Mwa ici Mulungu, ndiye Mulungu wanu, wakudzozani Ndi mafuta a cikondwerero ceni ceni koposa anzanu. Ndipo, Inu, Ambuye, paciyanbipo munaika maziko ace a dziko, Ndipo miyamba iri nchito ya manja anu; (Aefeso 1:9-11).

Baibulo limabvumbulutsa chinsinsi cha dongosolo la Mulungu ndi ichi ndiye mutu waukuru wa Baibulo. Baibulo ndi bvumbulutso la Yesu Khristu monga Mpulumutsi wa anthu onse. Yesu anafotokozera momwe Chipangano Chakale chinakhazikikira pa Iye:

Ndipo 7 anawatsegulira mitima yao, kuti adziwitse malembo; (Luka 24:45)

Ndi mau oyamba amenewa, Yesu anapitiriza kunena kuti:

ndipo anati kwa iwo, 8 Kotero kwalembedwa, kuti Kristu amve zowawa, nauke kwa akufa tsiku lacityatu; (Luka 24:46)

Zipangano zonse ziwiri zimakamba nkhani ya Yesu Khristu. Chipangano Chakale chimatikonzekeretsa ku zinthuzo zisanachitike pamene Chipangano Chatsopano chimatifotokozera momwe zinachitikira. Izi zinapangitsa kuti Baibulo likhale ndi mutu umodzi. Anthu omwe amayang’anira kubwera kwa Yesu m’Chipangano Chakale anapulumutsidwa ku machimo awo pa kukhulupirira lonjezano la Mulungu. Ndipo yense wakuyang’a m’mbuyo pa kukwaniritsidwa kwake mwa Yesu Khristu amapulumutsidwanso chimodzimodzi: Mwakukhulupirira kuti zinachitika monga mwa lonjezano la Mulungu.

KUSIYANA KWA BAIBULO

Tikamalankhula za “kusi yana” kwa Baibulo timatanthauza kuti Baibulo liri m’malembedwe osiyanasiyana. Limalemba mosiyanasiyana za momwe Mulungu anachitira ndi anthu komanso njira zosiyanasiyana za momwe anthuwo anachitira ndi Mulungu.

Baibulo lalembedwa mosiyanasiyana. Ndime zina zimaonetsa chimwemwe pamene zina zimaonetsera chisoni. Kalembedwe kake nkosiyanasiyananso. Muli mabuku a mbiri, ndakatulo, uneneri, makalata, nkhani, mafanizo, zozizwa, ndi nkhani za chikondi. Chifukwa cha kusi yana kotereku, mabuku a m’Baibulo agawidwa m’magulu akuruakuru.

MAGAWO A M’CHIPANGANO CHAKALE

Mabuku a m’Chipangano Chakale agawidwa m’magulu anayi akuruakuru: chilamulo, mbiri, ndakatulo ndi uneneri.

MABUKU A CHILAMULO:

Pali mabuku asanu a chilamulo ndipo maina awo ndi awa:

1. Genesisi
2. Eksodo
3. Levitiko
4. Numeri
5. Deuteronomu

Mabuku amenewa analemba za momwe Mulungu analengera dziko lapansi komanso munthu. Amafotokozeranso mbiri yoyambirira ya munthu. Mabukuwa amakamba momwe Mulungu anadzutsira dziko la Israel ngati mtundu womwe Mulungu adzagwiritse ntchito pakudzibvumbulutsa yekha ku anthu onse a dziko lapansi.

Mabuku amenewa mumapezeka malamulo a Mulungu. Odziwika bwino kwambiri ndi Malamulo Khumi a Mulungu (Eksodo 20:3-17); lamulo lalikuru kuposa onse (Deuteronomu 6:50, ndi lamulo lachiwiri ku lalikuru kuposa onse (Levitiko 19:28).

Tsegulani Baibulo lanu ndi kupeza mabuku a Chilamulo mu Chipangano Chakale. Pezani mavesi atatu omwe aperekedwa m’mwambawa ndi kuwawerenga. Mavesiwa ndi chitsanzo chabe cha malamulo a Mulungu omwe amapezeka m’ mabuku a Chilamulo.

MABUKU A MBIRI

Mu Chipangano Chakale muli mabuku okwanira 12 a mbiri. Maina a mabukuwa nawa:

Yoswa

Oweruza

Rute

1-2 Samuel

1-2 Mafumu

1-2 Mbiri

Ezra

Nehemiah

Estere

Pezani mabuku amenewa m’Baibulo lanu. Amapezeka mukangomaliza mabuku a Chilamulo. Mabukuwa amakamba za mbiri ya zaka chikwi ya anthu a Mulungu, Israel. Sikuti akukamba zonse zimene zidachitika mu nthawi imeneyi ayi, koma nkhani zikuluzikulu ndi zotsatira zake; zotsatira kapena kunyozera chilamulo cha Mulungu.

MABUKU A NDAKATULO

Pali mabuku okwana asanu a ndakatulo. Mabukuwa nawa:

Yobu

Masalimo

Miyambo

Mlaliki

Nyimbo ya Solomoni

Mabuku amenewa ndi mabuku a kupembedza kwa anthu a Mulungu, Israel. Amagwiritsidwabe ntchito ndi okhulupirira m’masiku ano nkupembedza. Tsegulani Masalimo 23 ndipo muwerenge. Ichi ndi chitsanzo chokongola cha ndakatulo zopembedza zomwe ziri m’ mabuku amenewa.

MABUKU A UNENERI

Mabuku a uneneri m’Chipangano Chakale agawidwa m’magulu awiri: Aneneri Akulu ndi Aneneri Aang’ono. Izi sizitanthauza kuti aneneri aakuluwa ndiye ofunika kwambiri kuposa enawo ayi. Kusiyana kwawo kumabwera pa matalikidwe a mabuku ena. Mabuku ena alemba zambiri ndipo ena alemba zochepa. Mabuku onse a uneneri m’Chipangano Chatsopano alipo 17 ndipo maina awo nawa:

Aneneri Aakulu

Yesaya

Yeremiya

Maliro

Ezekiel

Daniel

Aneneri Aang’ono

Hoseya

Nahum

Yoweli

Habakuku

Amosi

Zakariya

Obadiya

Haggai

Yona

Zekariya

Mika

Malaki

Mabuku amenewa ndi mauthenga a uneneri ochokera kwa Mulungu kupita kwa anthu ake za zomwe zichitike mtsogolo. Ambiri mwa mauneneriwa anakwaniritsidwa kale, koma ena saakwaniritsidwebe. Pezani mabuku auneneriwa m’Baibulo lanu. Mabukuwa ali kumapeto kwa Chipangano Chatsopano.

CHIPANGANO CHATSOPANO

Chipangano Chatsopano chagawidwanso m'magawo anayi: Mabuku a Uthenga Wabwino, Mbiri, Makalata ndi Uneneri.

MABUKU A UTHENGA WABWINO

Pali mabuku anayi a Uthenga Wabwino ndipo maina awo nawa:

Mateyu Marko Luka Yohane

Mabuku amenewa amakamba za moyo, kufa ndi kuuka kwa Yesu. Cholinga chake ndi kukutsogolerani inu kukhulupirira kuti Yesu ndi Khristu, Mwana wa Mulungu. Pezani pomwe pali mabuku a Uthenga Wabwino m'Baibulo mwanu kenako muwerenge Yohane 20:31 pomwenso pali cholinga cha mabuku a Uthenga Wabwino.

MABUKU A MBIRI

Mu Chipangano Chatsopano muli bukhu limodzi lokha la mbiri, Buku la Machitidwe. Bukhuli limafotokozero momwe mpingo unayambira ndi kukwaniritsa ntchito yaikulu yofalitsa Uthenga Wabwino padziko lonse lapansi. Pezani buku la Machitidwe m'Baibulo lanu.

MAKALATA

Makalata onse m'Chipangano Chatsopano amakwana 21. Ndipo maina awo nawa:

| | |
|---------------------|--------------------|
| Aroma | Tito |
| 1 ndi 2 Akorinto | Filemoni |
| Agalatiya | Ahebri |
| Aefeso | Yakobo |
| Afilipi | 1 ndi 2 Petro |
| Akolose | 1, 2, ndi 3 Yohane |
| 1 ndi 2 Atesalonika | Yuda |
| 1 ndi 2 Timoteyo | |

Makalatawa analembedwa kunka kwa okhulupirira ndi cholinga chowatsogolera kukhala moyo wauzimu ndi kuwathandiza kuchita zomwe Khristu anawalamulira. Aroma 12 ndi chitsanzo chabwino cha chiphunzitso cha m'makalata. Tsegulani chaputala chimenechi ndi kuchiwerenga.

UNENERI

Bukhu la Chibvumbulutso ndi bukhu lokhalo la uneneri m'Chipangano Chatsopano.

Limafotokozero za chigonjetso chomaliza cha Khristu Yesu pamodzi ndi anthu ake. Cholinga chake ndi cholimbikitsa okhulupirira kukhala moyo woyenera Akhristu kufikira chimaliziro cha nthawi ya pansi pano. Chibvumbulutso 2:10 ndiye chidule cha nkhani yonse m'bukhuli.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera osonera:

2. Kodi Mau oti “Baibulo” amanthauza chiyani?

3. Kodi mau oti “Malemba” amanthauza chiyani?

4. Kodi magawo awiri akuluakulu a m’Baibulo ndi ati?

5. Kodi m’Baibulo muli mabuku angati?

6. Tchulani magawo akuluakulu anayi amene mabuku a m’Chipangano Chakale agawidwamo.

7. Kodi mau oti “chipangano” amanthauza chiyani?

8. Kodi zolinga zenizeni zinayi za Baibulo ndi ziti? Perekani vesi yomwe ikuthandizira yankho lanu.

9. Kodi mau akuti “kugwirizana kwa Baibulo” amanthauza chiyani?

10. Kodi mau akuti “kusiyana kwa Baibulo” amanthauza chiyani?

11. Werengani ndime iriyonse. Lembani T kumayambiriro kwa ndime imene ikunena zoonza ndipo lembani F kumayambiriro a ndime imene ikunena zabodza.

- a. ___ Baibulo ndi mau olembedwa a Mulungu m’modzi woonza.
- b. ___ Ngakhale Mulungu anauzira mau ake koma anagwiritsa ntchito anthu kuti alembe Baibulo.
- c. ___ Popeza linalembedwa ndi anthu ambiri komanso nthawi yaitali, Baibulo liri ndi zotsutsana zambiri.
- d. ___ Baibulo ndi mabuku osiyanasiyana olankhula zosiyanasiyanso ndipo liribe mutu weni weni umodzi waukuru.
- e. ___ Aneneri Aakulu m’Baibulo ndi ofunika kwambiri kuposa Aneneri Aang’ono.

12. Kodi mabvumbulutso a m’zipangano zonse ziwiri amakhazikika pa ndani? Perekani vesi yothandizira yankho lanu_____

Vesi:

(Mayankho a mafunso onsewa ali kumapeto kwa bukhu lino)

KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

MAGAWO AKULU A BAIBULO

MABUKU A CHILAMULO:

GENESIS
EKSODO
LEVITIKO
NUMERI
DEUTERONOMO

MABUKU A MBIRI MU CHIPANGANO CHAKALE

YOSWA
OWERUZA
RUTE
I NDI II SAMUELI
I NDI II MAFUMU
I NDI II MBIRI
EZARA
NEHEMIYA
ESTERE

MABUKU A NDAKATULO:

MASALMO
MIYAMBO
MLALIKI
NYIMBO YA SOLOMONI

MABUKU A UNENERI MU CHIPANGANO CHAKALE:

ANENERI A AKULU:

YESAYA
YEREMIYA
MALIRO
EZEKIELI
DANIYELI

ANENERI A ANG'ONO

| | |
|---------|----------|
| HOSEYA | NAHUMU |
| YOWELI | HABAKUKU |
| AMOSI | ZEFANIYA |
| OBADIYA | HAGAI |
| YONA | ZAKALIYA |
| MIKA | MALAKI |

MAKALATA A CHIPANGANO CHATSOPANO:

AROMA

I NDI II AKORINTO

AGALATIYA

AEFESO

AFILUPI

AKOLOSE

I NDI II ATESALONIKA

I NDI II TIMOTEO

TITO

FILEMONI

AHEBRI

YAKOBO

I NDI II PETRO

I, II NDI III YOHANE

YUDA

CHAPUTALA 2

MABUKU A M'BAIBULO

ZOLINGA

Mukamaliza phunziro muzikwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kuzindikira chiwerengero cha mabuku a m'Chipangano Chakale.
- Kuzindikira chiwerengero cha mabuku a m'Chipangano Chatsopano.
- Kufotokozero bwino kufunikira kokhala ndi dongosolo la kawerengedwe ka Baibulo.
- Kulemba zinthu zinayi zofunika m'kawerengedwe kabwino ka Baibulo.

VESI LOTSOGOLERA

Kupfuula kwanga kuyandikire pamaso pano, Yehova; Mundizindikiritse monga mwa mau anu. (Masalimo 119:169).

Mu chaputala chapitachi mwaphunzira kuti Baibulo ndi Mau olembedwa a Mulungu. Mwaphunziranso kuti Baibulo lagawidwa m'magawo awiri akuluakulu otchedwa Chipangano Chakale ndi Chipangano Chatsopano. Mwaona kalenso za magawo anayi a mabuku a m'Chipangano Chakale:

Chilamulo

Mbiri

Ndakatulo

Uneneri

Mwaphunzira za magawo anayi a mabuku a m'Chipangano Chatsopano:

Mabuku a Uthenga Wabwino

Mbiri

Makalata

Uneneri

Umu ndi momwe mabuku aliri:

| | |
|--------------------------------|------------------------------|
| BAIBULO | |
| MAU OLEMBEDWA A MULUNGU | |
| MABUKU 66 | |
| CHIPANGANO CHAKALE | CHIPANGANO CHATSOPANO |
| Chilamulo | Mabuku a Uthenga Wabwino |
| Mbiri | Mbiri |
| Ndakatulo | Makalata |
| Uneneri | Uneneri |

Chaputala chino chifotokozera mwachidule nkhani zopezeka mu mabuku onse 66 a m’Baibulo omwe amapanga Chipangano Chakale ndi Chatsopano. Chikupereka mau otsogolera a magawo awiri komanso zinthu zinayi zomwe mungagwiritse ntchito kuti kuwerenga Baibulo kwani kukhale kopambana. Ndipo mudzasankha njira dongosolo la tsatanetsatane lomwe muzigwiritsa ntchito powerenga Baibulo.

CHIPANGANO CHAKALE (MABUKU 39)

MABUKU A CHILAMULO

Genesisi: Amafotokoza za chiyambi cha dziko, munthu, Sabata, ukwati, banja, tchimo, nsembe, maiko, ndi kayendetsedwe ka zinthu komanso ziphona za Mulungu monga Abraham, Isaki, Yakobo ndi Yosefe.

Eksodo: Limafotokozera momwe Israel anakhalira dziko ndi Mose kukhala mtsogoleri. Israel kumasulidwa ku ukapolo m’Aigupto ndi kuyenda kunka ku phiri la Sinai kumene Chilamulo chinaperekedwa.

Levitiko: Ili ndi bukhu la chipembedzo cha Chiyuda. Liri ndi malangizo a atsogoleri a chipembedzo ndipo limafotokoza momwe anthu ochimwa angabwerere pamaso pa Mulungu wolungama. Ndipo limalozera kukubwera kwa Khristu Yesu ngati mwana wa nkhusa wa Mulungu yemwe amatchotsa tchimo la anthu a dziko lapansi.

Numeri: Bukuli linalamba za ana a Israel akuzungulira m'chipululu kwa zaka 40 ngati zotsatira za kusamvera Mulungu. Dzinali linachokera pa kalemba muwiri yemwe anachitika mkatikati mwa ulendo wautaliu.

MABUKU A MBIRI

Yoswa: Limafotokoza tsatanetsatane wa momwe Yoswa, mlowa m'malo wa Mose, anatsogolerera Israel kulowa m'dziko la malonjezano la Kenani. Komanso muli nkundo zimene zinamenyedwa ndi kagawidwe ka dziko pakati pa anthu onse.

Oweruza: Israel wachoka pamaso a Mulungu Yoswa atangomwalira. Bukhuli limafotokoza nkhanu yomvetsa chisoni ya uchimo womwe unakhathamira pa Israel ndi kuikidwa kwa oweruza omwe Mulungu amadzutsa kuti aombole ana a Israel ku mphamvu za adani awo.

Rute: Nkhani ya Rute, mkazi wochokera ku dziko la mitundu la Moabu, yemwe anasankha kutumikira Mulungu wa Israel. Anakhala kholo la Davide.

1 Samuel: Buku ili linakhazikika pa anthu atatu: Samuel yemwe anali woweruza womaliza wa Israel; Sauli, mfumu yoyamba ya Israel; ndi Davide yemwe analowa m'malo mwa Sauli ngati mfumu.

2 Samuel: Ulamuliro wopambana wa Davide wa zaka 40 ukukambidwa m'bukhu limeneli.

1 Mafumu: Nkhani zazikulu m'bukuli ndi za ulamuliro wa Solomoni komanso mafumu a ufumu wogawikana wa Israel ziri m'bukhu limeneli. Ahabu kumpoto ndi Yehosafati kumwera.

2 Mafumu: Kugwa komalizira kwa Israel ndi Yuda kwalembedwa m'bukhu limeneli. Anthu a Mulungu anagwa mu uchimo wazama kwambiri.

1 Mbiri: Ulamuliro wa Davide ndi kukonzekera kumangidwa kwa kachisi ziri m'menemu. Bukhuli linalembedwa nthawi yofanana ndi 2 Samuel.

2 Mbiri: Bukhuli limafotokozera za mbiri ya Israel m'nthawi ya ulamuliro wa Solomoni makamaka ufumu wa kumwera. Likumalizika ndi lamulo Sirasi yemwe analamulira kuti anthu a Mulungu abwerere kwao ku Yerusalemu kuchoka ku Babulo.

Estere: Kuombedwa kwa anthu a Mulungu kudzera mwa Estere ndi Modekai ndiye nkhani zikuluzikulu za bukhuli.

MABUKU A NDAKATULO

Yobu: Buku ili ndi nkhani ya Yobu, munthu yemwe anakhala pafupifupi nthawi ya Abrahamu. Nkhani yaikulu m'bukhuli ndi funso lakuti chifukwa chiyani okhulupirira amakumana ndi zowawa.

Masalimo: Bukhu la pemphero ndi matamando m'Baibulo.

Miyambo: Nzeru za Umulungu pothana ndi mavuto a m'moyo uno a tsiku ndi tsiku.

Mlaliki: Bukhuli limakamba mosaphyatira kuti moyo wopanda Mulungu ndi wopanda pake.

Nyimbo ya Solomoni: Chikondi cha mfumu Solomoni pa mkazi wake waku Sulemu. Nkhaniyi imaimilira chikondi cha Mulungu pa Israel ndi cha Khristu pa mpingo.

MABUKU A UNENERI

Mabuku angapo a ndakatulo analembedwa mu nthawi imene ufumu wa Israel unagawika pawiri. Israel ndi Yuda.

Yesaya: Akuchenjeza za chilango chomwe chinkabwera pa Israel chifukwa cha kumchimwira Mulungu.

Yeremiya: Linalembedwa cha kumapeto kwa kugwa kwa Yuda. Analankhula za chilango chiri nkuza ndipo analimbikitsa anthu kuti agonjere kwa Nebukadinezara.

Maliri: Kulira kwa Yeremiya chifukwa cha kuonongedwa kwa Yerusalemu ndi anthu a ku Babulo.

Ezekiel: Poyamba akuchenjeza za kugwa kwa Yerusalemu kenako kubwezeretsedwa kwake.

Daniel: Mneneri Daniel anagwidwa ukapolo kunka ku Babulo nthawi imene Yuda anathiridwa. Bukhuli likupereka chiphunzitsa cha mbiri komanso uneneri chomwe ndi chofunika kwambiri pa kumvetsa uneneri wa m'Baibulo.

Hosea: Mutu waukulu m'bukhuli ndi kusakhulupirika kwa Israel, kulangidwa ndi kubwezeretsedwa kwao ndi Mulungu.

Yoeli: Akukamba za miriri yomwe imaimilira chilango cha mtsogolo.

Amosi: Iyi inali nthawi yochita bwino mu chuma pamene chikhalidwe chinali chowola. Amosi anachenjeza Israel ndi maiko ozungulira za chilango cha Mulungu pa tchimo lawo.

Obadiya: Chiweruzo cha Mulungu pa Edom, dziko loipa kumwera kwa Nyanja Yakufa.

Yonah: Nkhani ya Mneneri Yona amene analalikira za kulapa mu mzinda wa Nineve, likulu la ufumu wa Asiriya. Bukhuli likubvumbulutsa za chikondi cha Mulungu ndi dongosolo lake la chipulumutso kwa Amitundu.

Mika: Uneneri wina wotsutsana ndi tchimo la Israel. Akuneneratu za malo omwe Yesu adzabadwire padakali zaka 700 kuti zimenezi zichitike.

Nahum: Akunenera za kuonongedwa kwa Nineve mzinda womwe Mulungu anausiya osononga 150 zapitazo utalapa pamene Yona analalikira.

Habakuku: Akubvumbulutso dongosolo la Mulungu lolanga dziko lochimwa pogwiritsa ntchito dziko lina lochimwanso kwambiri. Bukhuli limaphunzitsa kuti, “olungama adzakhala ndi moyo ndi chikhulupiriro.”

Zefaniya: Kuweruzidwa ndi kubwezeretsedwa kwa Yuda.

Hagai: Akupempha Ayuda kuti amangenso kachisi patadutsa zaka 15 zochedwa kumanga chifukwa cha mantha pa adani.

Zekariya: Akupemphabe kuti amalize kachisi ndi kuikanso moyo wauzimu m'malo.

Akuneneranso za kubwera kwa Yesu koyamba komanso kwachiwiri.

Malaki: Akuchenjeza za kusadzipereka kwatunthu kwa Mulungu ndi kuneneranso za kubwera kwa Yohane Mbatizi ndi Yesu.

CHIPANGANO CHATSOPANO (MABUKU 27)

MABUKU A UTHENGA WABWINO

Mabuku anayi a Uthenga Wabwino akufotokozera za kubadwa, moyo, utumiki, ziphunzitsso, imfa, ndi kuuka kwa Yesu Khristu. Mabuku amasiyana mkalembedwe.

Mateyu: Akutsindika kwambiri za Khristu ngati Mfumu ndipo analembereka kwambiri kwa Ayuda.

Marko: Akutsindika za Yesu ngati Kapolo wa Mulungu ndipo akupita kwa anthu a ku Roma.

Luka: Akufotokozera za Yesu ngati “Mwana wa Munthu,” mpulumutsi wamngwiro wa anthu ochimwa.

Yohane: Akumuika Yesu pa malo ake ngati Mwana wa Mulungu.

BUKHU LA MBIRI

Machitidwe a Atumwi: Bukhu la mbiri m’Chipangano Chatsopano linalemba za momwe mpingo unakulira kuyambira nthawi imene Yesu anakwera kunka kumwamba mpakana kumangidwa kwa Paulo kwa Aroma. Bukhuli likukamba za nkhani zochitika mu zaka 33 ndi kutsindika kwambiri za ntchito ya Mzimu Woyera.

MAKALATA

Aroma: Iyi ndi kalata yomwe ikukamba za Uthenga Wabwino ndi kutsindika kwambiri za chipulumutso kudzera m’chikhulupiriro basi.

1 Akorinto: Inalembedwa kukakonza zolakwika m’chikhalidwe cha Chikhristu ku mpingo wa ku dera.

2 Akorinto: Akulankhula za utumiki weniweni wa Uthenga Wabwino, kukhulupirika pa zinthu, ndi za ulamuliro wa utumwi wa Paulo.

Agalatiya: Akulimbana kwambiri za mchitidwe wosakaniza chilamulo ndi chikhulupiriro. Mutu wa bukhu ndi kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro.

Aefeso: Akulimbikitsa okhulupirira za malo awo mwa Khristu.

Afilipi: Akutsindika kwambiri za chimwemwe cha umodzi wa Akhristu.

Akolose: Akulimbana kwambiri ndi chiphunzitso chomwe chinakana kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu. Bukhuli likutsindikanso kuti Yesu ndiye mutu wa mpingo.

1 Atesalonika: Amalangiza za moyo wa Chikristu ndi kutsindika za kubweranso kwa Yesu Khristu.

2 Atesalonika: Kupitiriza nkhani ya kubweranso kwa Ambuye ndi momwe kudziwa izi kungathandizire kukhala moyo woyenera.

1 Timoteyo: Amatsindika chiphunzitso cholamitsa, dongosolo loyenera la mu mpingo, ndi mfundo zothandizira mpingo kuyenda bwino mtsogolomu.

2 Timoteyo: Akufotokozera za kapolo weni weni wa Yesu Khristu. Bukhuli limachenjezanso za kubwelera m'mbuyo moyo wauzimu komwe kunali kutayamba. Limationetsera kuti Mau a Mulungu ndi njira yokhayo yothana ndi ziphunzitso zonama.

Tito: Uyu ndi kalata wa Paulo kwa mtumiki wachinyamata wotchedwa Tito yemwe amatumikira Mulungu pa chilumba cha Krete. Chiphunzitso cholamitsa ndi moyo wa Umulungu zatsindikidwanso m'bukhuli.

Filemoni: Paulo kupembedzera za kapolo wothawa wa Mkhristu wina wolemera wa ku Kolose. Kalatayu akupereka chithunzi cha Yesu m'malo mwa wokhulupirira yemwe anali kapolo wa uchimo.

Ahebri: Akufotokozera za kupambana kwa Chikristu kuposa Chiyuda. Bukhuli limafotozera za Yesu monga Mkulu Wansembe Wamkulu ndi mkhalapati wa Mulungu ndi munthu.

Yakobo: Amaphunzitsa kuti chikhulupiriro chenicheni chimayenera kukhala ndi ntchito, ngakhale chipulumutso chimabwera mwa chikhulupiriro basi.

1 Petro: Kalata wa chithonhozo ndi chilimbikitso kwa okhulupirira, makamaka iwo akukumana ndi nkondo zauzimu kudzera mwa osakhulupirira.

2 Petro: Chenjezo pa nkondo zauzimu kuchokera mkati mwa mpingo. Mwachitsanzo, aphunzitsi onyenga omwe anali "atalowa" kale mu mpingo.

1 Yohane: Kalatayi inalembedwa kulimbana ndi chiphunzitso chokana kuti Khristu ndi Mwana wa Mulungu komanso Mwana wa Munthu. Bukhuli limatsindika chiyanjano ndi chikondi pakati pa okhulupirira. Limatsimikiziranso okhulupirira za moyo wosatha.

2 Yohane: Limachenjeza kunyengelera chiphunzitso chonama ndi kutsindika kuti choonadi chikuyenera kuyang'aniridwa ndi chikondi chonse.

3 Yohane: Limachenjeza za tchimo lokana kuyanjana ndi okhulupirira eni eni.

Yuda: Bukhu linanso lochenjeza za kubwerera m'mbuyo moyo wauzimu ndi ziphunzitso zonyenga. Mutu wake ndi wofanana ndi wa 2 Petro.

BUKHU LA UNENERI

Chibvumbulutso: Bukhu la uneneri ili limafotokozerwa za chimaliziro cha zochitika za padziko lapansi. Limakamba za zinthu zomwe zinali, ziri komanso zomwe zidzakhalepo mu dongosolo la Mulungu la mtsogolo.

KAWERENGEDWE KABWINO KA BAIBULO

M'maphunziro ano muphunzira za momwe mungamvetsere ndi kumasulira bwino Baibulo. Muphunziranso njira zakasanthulidwe ka Baibulo mwa luso. Komano kumvetsa bwino Baibulo kumayamba nkuti munthu aliwerenge Baibulolo. Kuti tikuthandizeni kuwerenga bwino Mau a Mulungu, taika madongosolo angapo osiyanasiyana owerengera Baibulo. Madongosolowa akuphatikizapo omwe angathandize anthu amene akuyamba kumene kuwerenga Mau a Mulungu komanso amkhala kale pa kawerengedwe ka Mau a Mulungu. Poyamba, pali njira njira zinayi izi zomwe mutha kutsata mkawerengedwe kabwino ka Baibulo.

1. WERENGANI TSIKU NDI TSIKU:

Komatu m'cilamulo ca Yehova muli cikondwerero cace; Ndipo m'cilamulo cace amalingima usana ndi usiku. (Masalimo 1:2)

Mulungu anapanga thupi lanulo ndipo mukuyenera kumadya tsiku ndi tsiku kuti mukhale athanzi. Chimodzimidzinsu, mzimu wanu akuyenera kupatsidwa chakudya cha Mau a Mulungu kuti mukhale athanzi muuzimu.

.... kwalembedwa, munthu sadzakhala ndi moyo ndi mkate wokha koma ndi mau onse oturuka mkamwa mwa Mulungu (Luka 4:4).

2. WERENGANI MOSANKHULA

Yambani ndi “mkaka” wa mau kuwerenga. Izi ndi ziphunzitso zosavuta m'Mau a Mulungu:

Ndipo ambiri adzatsata zonyansa zao; cifukwa ca iwo njira ya coonadi idzanenedwa zamwano. (1 Petro 2:2)

Kenaka mukhwima muuzimu kufika pa mlingo wotha kudya “nyama” ya Mau a Mulungu. Kutanthauza kuti muyamba kumvetsa tsopano ziphunzitso zovutirapo za m’Mau a Mulungu:

Pakuti yense wakudya mkaka alibe cizolowezi ca mau a cilungamo; pakuti ali khanda. Koma cakudya cotafuna ciri ca anthu akulu misinkhu, amene mwa kucita nazo anazoloweretsa zizindikiritso zao kusiyanita cabwino ndi coipa.

(Ahebri 5:13-14)

Ndinaiyetsa inu mkaka, si cakudya colimba ai; pakuti simunaeikhoza; ngakhale tsopano lino simucikhoza; pakuti mulinso athupi; (1 Akorinto 3:2)

3. WERENGANI MWA PEMPHERO

Pakuti Ezra anakonzekeretsa mtima wake kufunafuna chilamulo cha Ambuye (Ezra 7:10)

Musanayambe kuwerenga, pempherani kumfunsa Ambuye kuti akuthandizeni kumvetsa uthenga womwe akukupatsani kudzera m’Mau ake olembedwawa. Pemphero lanu likhale monga la Davide:

(Masalimo 119:18)

4. WERENGANI MWA DONGOSOLO

Anthu ambiri satha kumvetsa Mau a Mulungu chifukwa chakuti alibe dongosolo labwino lowerengera. Amawerenga chaputala ichi lero, akawerenga chinanso uko mawa ndipo amakanika kulumikiza nkhani zomwe akuwerenga. Izi ziri ngati kuwerenga zinthu zaumoyo mwa apa ndi apo basi kenako nkuyambitsa chipatala. Baibulo limatiuza kuti “tifufuze malemba” (Yohane 5:39). Kutanthauza kuwerenga Mau mosamalitsa. Baibulo liri ngati bukhu lophunzirira mkalasi. Limayenera kuwerengedwa mwatsatanetsatane kuyambira kumayambiliro mpakana kumapeto kuti mumvetse zinthu zimene zalembedwamo. Sankhani limodzi mwa madongosolo owerengera Mau omwe ali m’musiwa ndipo muyambe kuwerenga Baibulo lanu tsiku ndi tsiku.

KWA ONGOYAMBA KUMENE

Ngati simunawerengepo Baibulo chiyambire, yambani ndi Bukhu la Yohane m'Chipangano Chatsopano. Bukhu limeneli linalembedwa ndi m'modzi mwa ophunzira a Yesu wotchedwa Yohane. Amafotokozerana nkhani ya Yesu mu njira yosavuta kumvetsa.

Werengani chaputala chimodzi m'bukhuli tsiku liri lonse mwatsatanetsatane, osadumphira machaputala. Gwiritsani ntchito katchati kali m'musimu ndipo muzichonga mukawerenga tsiku lirilonse.

Uthenga wa Bwino wa Yohane:

_____ 1 _____ 5 _____ 9 _____ 13 _____ 17

_____ 2 _____ 6 _____ 10 _____ 14 _____ 18

_____ 3 _____ 7 _____ 11 _____ 15 _____ 19

_____ 4 _____ 8 _____ 12 _____ 16 _____ 20

DONGOSOLO LALIFUPI

Njira iyi ya kawerengedwe ka Mau inakonzedwa kuti ipereke chidziwitso chapamwamba cha Baibulo kudzera m'ndime zosankhika za Malemba. Werengani ndimezi mu mndandanda womwe aziikira. Gwiritsani ntchito tchati chili m'musichi ndipo muzichonga mukawerenga gawo limenelo:

CHIPANGANO CHATSOPANO:

_____ Yohane _____ 1 Atesalonika _____ Aefeoso

_____ Marko _____ 1 Akorinto _____ 2 Timoteyo

_____ Luka _____ Aroma _____ 1 Petro

_____ Machitidwe _____ Filimoni _____ 1 Yohane

_____ Aroma _____ Afilipi _____ Chibvumbulutso 1-5; 19:6-22:21

CHIPANGANO CHAKALE:

_____ Genesis _____ Amosi

_____ Eksodo 1-20 _____ Yesaya 1-12

_____ Numeri 10:11-21:35 _____ Yeremiya 1-25;39-33

| | |
|--------------------------------------|-----------------------|
| _____Deuteronomu 1-II | _____Rute |
| _____Yoswa 1-12; 22-24 | _____Yona |
| _____Oweruza 1-3 | _____Masalimo 1-23 |
| _____1 Samuel 1-3, 9-10,1 3,15-18,31 | _____Yobu 1-14, 38-42 |
| _____2 Samuel 1 | _____Miyambo 1-9 |
| _____1 Mafumu 1-II | _____Daniel 1-6 |
| _____Nehemiya | |

DONGOSOLO LALITALI

Dongosolo ili limalowa kwakuya ndithu kuposa Dongosolo Lalifupi, komabe silitenga Baibulo lonse

CHIPANGANO CHATSOPANO

| | |
|--------------------|-----------------|
| _____Marko | _____Afilipi |
| _____Mateyu | _____Aefeso |
| _____Yohane | _____2 Timoteyo |
| _____Luka | _____Tito |
| _____Machitidwe | _____1 Timoteyo |
| _____1 Atesalonika | _____1 Petro |
| _____2 Atesalonika | _____Ahebri |
| _____1 Akorinto | _____Yakobo |
| _____2 Akorinto | _____1 Yohane |
| _____Agalatiya | _____2 Yohane |
| _____Aroma | _____3 Yohane |
| _____Filimoni | _____Yuda |
| _____Akolose | _____2 Petro |

_____ Chibvumbulutso 1-5 ndi 19:6-22:21

CHIPANGANO CHAKALE

_____ Genesesi

_____ Yeremiya 1-25 ndi 30-33

_____ Eksodo 1-24

_____ Nahumu

_____ Levitiko 1-6:7

_____ Habakuku

_____ Numeri 10:11-21:35

_____ Ezekiel 1-24 ndi 33-39

_____ Deuteronomu 1-II ndi 27-34

_____ Obadiya

_____ Yoswa 1-12 ndi 22-24

_____ Maliro

_____ Oweruza 1-16

_____ Yesaya 40-66

_____ 1 Samueli

_____ Zekariya 1-8

_____ 2 Samueli

_____ Malaki

_____ 1 Mafumu

_____ Yoweli

_____ 2 Mafumu

_____ Rute

_____ 1 Mbiri

_____ Yona

_____ 2 Mbiri

_____ Masalimo

_____ Ezra

_____ Yobu

_____ Nehemiya

_____ Miyambo 1-9

_____ Amosi

_____ Nyimbo ya Solomo

_____ Hosea

_____ Mlaliki

_____ Mika

_____ Estere

_____ Yesaya 1-12

_____ Daniel

_____ Zefaniya

DONGOSOLO LA CHAKA CHONSE

Dongosololi limakutengerani chaka chonse kuti mumalize:

The complete Bible reading schedule takes you through the entire Bible in one year.

| January | | February | |
|----------------|----------------|-----------------|----------------|
| ____1. | Genesesi 1-2 | ____1. | Eksodo 14-17 |
| ____2. | Genesesi 3-5 | ____2. | Eksodo 18-20 |
| ____3. | Genesesi 6-9 | ____3. | Eksodo 21-24 |
| ____4. | Genesesi 10-11 | ____4. | Eksodo 25-27 |
| ____5. | Genesesi 12-15 | ____5. | Eksodo 28-31 |
| ____6. | Genesesi 16-19 | ____6. | Eksodo 32-34 |
| ____7. | Genesesi 20-22 | ____7. | Eksodo 35-37 |
| ____8. | Genesesi 23-26 | ____8. | Eksodo 38-40 |
| ____9. | Genesesi 27-29 | ____9. | Levitiko 1-4 |
| ____10. | Genesesi 30-32 | ____10. | Levitiko 5-7 |
| ____11. | Genesesi 33-36 | ____11. | Levitiko 8-10 |
| ____12. | Genesesi 37-39 | ____12. | Levitiko 11-13 |
| ____13. | Genesesi 40-42 | ____13. | Levitiko 14-16 |
| ____14. | Genesesi 43-46 | ____14. | Levitiko 17-19 |
| ____15. | Genesesi 47-50 | ____15. | Levitiko 20-23 |
| ____16. | Yobu 1-4 | ____16. | Levitiko 24-27 |
| ____17. | Yobu 5-7 | ____17. | Numeri 1-3 |
| ____18. | Yobu 8-10 | ____18. | Numeri 4-6 |
| ____19. | Yobu 11-13 | ____19. | Numeri 7-10 |
| ____20. | Yobu 14-17 | ____20. | Numeri 11-14 |
| ____21. | Yobu 18-20 | ____21. | Numeri 15-17 |
| ____22. | Yobu 21-24 | ____22. | Numeri 18-20 |

- | | | | |
|----------|--------------|----------|-----------------|
| _____23. | Yobu 25-27 | _____23. | Numeri 21-24 |
| _____24. | Yobu 28-31 | _____24. | Numeri 25-27 |
| _____25. | Yobu 32-34 | _____25. | Numeri 28-30 |
| _____26. | Yobu 35-37 | _____26. | Numeri 31-33 |
| _____27. | Yobu 38-42 | _____27. | Numeri 34-36 |
| _____28. | Eksodo 1-4 | _____28. | Deuteronomu 1-3 |
| _____29. | Eksodo 5-7 | | |
| _____30. | Eksodo 8-10 | | |
| _____31. | Eksodo 11-13 | | |

March

April

- | | | | |
|----------|-------------------|----------|-----------------|
| _____1. | Deuteronomu 4-6 | _____1. | I Samuel 21-24 |
| _____2. | Deuteronomu 7-9 | _____2. | I Samuel 25-28 |
| _____3. | Deuteronomu 10-12 | _____3. | I Samuel 29-31 |
| _____4. | Deuteronomu 13-16 | _____4. | II Samuel 1-4 |
| _____5. | Deuteronomu 17-19 | _____5. | II Samuel 5-8 |
| _____6. | Deuteronomu 20-22 | _____6. | II Samuel 9-12 |
| _____7. | Deuteronomu 23-25 | _____7. | II Samuel 13-15 |
| _____8. | Deuteronomu 26-28 | _____8. | II Samuel 16-18 |
| _____9. | Deuteronomu 29-31 | _____9. | II Samuel 19-21 |
| _____10. | Deuteronomu 32-34 | _____10. | II Samuel 22-24 |
| _____11. | Yoswa 1-3 | _____11. | Masalimo 1-3 |
| _____12. | Yoswa 4-6 | _____12. | Masalimo 4-6 |
| _____13. | Yoswa 7-9 | _____13. | Masalimo 7-9 |
| _____14. | Yoswa 10-12 | _____14. | Masalimo 10-12 |

| | | | |
|--------|----------------|--------|----------------|
| ___15. | Yoswa 13-15 | ___15. | Masalimo 13-15 |
| ___16. | Yoswa 16-18 | ___16. | Masalimo 16-18 |
| ___17. | Yoswa 19-21 | ___17. | Masalimo 19-21 |
| ___18. | Yoswa 22-24 | ___18. | Masalimo 22-24 |
| ___19. | Oweruza 1-4 | ___19. | Masalimo 25-27 |
| ___20. | Oweruza 5-8 | ___20. | Masalimo 28-30 |
| ___21. | Oweruza 9-12 | ___21. | Masalimo 31-33 |
| ___22. | Oweruza 13-15 | ___22. | Masalimo 34-36 |
| ___23. | Oweruza 16-18 | ___23. | Masalimo 37-39 |
| ___24. | Oweruza 19-21 | ___24. | Masalimo 40-42 |
| ___25. | Rute 1-4 | ___25. | Masalimo 43-45 |
| ___26. | I Samuel 1-3 | ___26. | Masalimo 46-48 |
| ___27. | I Samuel 4-7 | ___27. | Masalimo 49-51 |
| ___28. | I Samuel 8-10 | ___28. | Masalimo 52-54 |
| ___29. | I Samuel 11-13 | ___29. | Masalimo 55-57 |
| ___30. | I Samuel 14-16 | ___30. | Masalimo 58-60 |
| ___31. | I Samuel 17-20 | | |

May

| | |
|-------|----------------|
| ___1. | Masalimo 61-63 |
| ___2. | Masalimo 64-66 |
| ___3. | Masalimo 67-69 |
| ___4. | Masalimo 70-72 |
| ___5. | Masalimo 73-75 |
| ___6. | Masalimo 76-78 |

June

| | |
|-------|---------------|
| ___1. | Miyambo 1-3 |
| ___2. | Miyambo 4-7 |
| ___3. | Miyambo 8-11 |
| ___4. | Miyambo 12-14 |
| ___5. | Miyambo 15-18 |
| ___6. | Miyambo 19-21 |

| | | | |
|--------|------------------|--------|-------------------------------|
| ___7. | Masalimo 79-81 | ___7. | Miyambo 22-24 |
| ___8. | Masalimo 82-84 | ___8. | Miyambo 25-28 |
| ___9. | Masalimo 85-87 | ___9. | Miyambo 29-31 |
| ___10. | Masalimo 88-90 | ___10. | Mlaliki 1-3 |
| ___11. | Masalimo 91-93 | ___11. | Mlaliki 4-6 |
| ___12. | Masalimo 94-96 | ___12. | Mlaliki 7-9 |
| ___13. | Masalimo 97-99 | ___13. | Mlaliki 10-12 |
| ___14. | Masalimo 100-102 | ___14. | Nyimbo 1-4 |
| ___15. | Masalimo 103-105 | ___15. | Nyimbo 5-8 |
| ___16. | Masalimo 106-108 | ___16. | I Mafumu 5-7 |
| ___17. | Masalimo 109-111 | ___17. | I Mafumu 8-10 |
| ___18. | Masalimo 112-114 | ___18. | I Mafumu 11-13 |
| ___19. | Masalimo 115-118 | ___19. | I Mafumu 14-16 |
| ___20. | Masalimo 119 | ___20. | I Mafumu 17-19 |
| ___21. | Masalimo 120-123 | ___21. | I Mafumu 20-22 |
| ___22. | Masalimo 124-126 | ___22. | II Mafumu 1-3 |
| ___23. | Masalimo 127-129 | ___23. | II Mafumu 4-6 |
| ___24. | Masalimo 130-132 | ___24. | II Mafumu 7-10 |
| ___25. | Masalimo 133-135 | ___25. | II Mafumu 11-14:20 |
| ___26. | Masalimo 136-138 | ___26. | Yoweli 1-3 |
| ___27. | Masalimo 139-141 | ___27. | II Mafumu 14:21-25; Yona 1-4 |
| ___28. | Masalimo 142-144 | ___28. | II Mafumu 14:26-29; Amosi 1-3 |
| ___29. | Masalimo 145-147 | ___29. | Amosi 4-6 |
| ___30. | Masalimo 148-150 | ___30. | Amosi 7-9 |

____31. I Kings 1-4

July

____1. II Mafumu 15-17

____2. Hoseya 1-4

____3. Hoseya 5-7

____4. Hoseya 8-10

____5. Hoseya 11-14

____6. II Mafumu 18-19

____7. Yesaya 1-3

____8. Yesaya 4-6

____9. Yesaya 7-9

____10. Yesaya 10-12

____11. Yesaya 13-15

____12. Yesaya 16-18

____13. Yesaya 19-21

____14. Yesaya 22-24

____15. Yesaya 25-27

____16. Yesaya 28-30

____17. Yesaya 31-33

____18. Yesaya 34-36

____19. Yesaya 37-39

____20. Yesaya 40-42

____21. Yesaya 43-45

August

____1. II Mafumu 20-21

____2. Zephaniah 1-3

____3. Habakkuk 1-3

____4. II Mafumu 22-25

____5. Obadiya/Yeremiya 1-2

____6. Yeremiya 3-5

____7. Yeremiya 6-8

____8. Yeremiya 9-12

____9. Yeremiya 13-16

____10. Yeremiya 17-20

____11. Yeremiya 21-23

____12. Yeremiya 24-26

____13. Yeremiya 27-29

____14. Yeremiya 30-32

____15. Yeremiya 33-36

____16. Yeremiya 37-39

____17. Yeremiya 40-42

____18. Yeremiya 43-46

____19. Yeremiya 47-49

____20. Yeremiya 50-52

____21. Maliro 1-5

| | | | |
|---------|--------------|---------|---------------|
| ____22. | Yesaya 46-48 | ____22. | I Mbiri 1-3 |
| ____23. | Yesaya 49-51 | ____23. | I Mbiri 4-6 |
| ____24. | Yesaya 52-54 | ____24. | I Mbiri 7-9 |
| ____25. | Yesaya 55-57 | ____25. | I Mbiri 10-13 |
| ____26. | Yesaya 58-60 | ____26. | I Mbiri 14-16 |
| ____27. | Yesaya 61-63 | ____27. | I Mbiri 17-19 |
| ____28. | Yesaya 64-66 | ____28. | I Mbiri 20-23 |
| ____29. | Micah 1-4 | ____29. | I Mbiri 24-26 |
| ____30. | Micah 5-7 | ____30. | I Mbiri 27-29 |
| ____31. | Nahum 1-3 | ____31. | II Mbiri 1-3 |

September

| | |
|---------|----------------|
| ____1 | II Mbiri 4-6 |
| ____2. | II Mbiri 7-9 |
| ____3. | II Mbiri 10-13 |
| ____4. | II Mbiri 14-16 |
| ____5. | II Mbiri 17-19 |
| ____6. | II Mbiri 20-22 |
| ____7. | II Mbiri 23-25 |
| ____8. | II Mbiri 26-29 |
| ____9. | II Mbiri 30-32 |
| ____10. | II Mbiri 33-36 |
| ____11. | Ezekiel 1-3 |
| ____12. | Ezekiel 4-7 |
| ____13. | Ezekiel 8-11 |

October

| | |
|---------|--------------------------|
| ____1. | Estere 4-7 |
| ____2. | Estere 8-10 |
| ____3. | Ezra 1-4 |
| ____4. | Haggai 1-2/Zechariya 1-2 |
| ____5. | Zechariya 1-2 |
| ____6. | Zechariya 3-6 |
| ____7. | Zechariya 7-10 |
| ____8. | Ezra 5-7 |
| ____9. | Ezra 8-10 |
| ____10. | Nehemiya 1-3 |
| ____11. | Nehemiya 4-6 |
| ____12. | Nehemiya 7-9 |
| ____13. | Nehemiya 10-13 |

____14. Ezekiel 12-14
____15. Ezekiel 15-18
____16. Ezekiel 19-21
____17. Ezekiel 22-24
____18. Ezekiel 25-27
____19. Ezekiel 28-30
____20. Ezekiel 31-33
____21. Ezekiel 34-36
____22. Ezekiel 37-39
____23. Ezekiel 40-42
____24. Ezekiel 43-45
____25. Ezekiel 46-48
____26. Daniel 1-3
____27. Daniel 4-6
____28. Daniel 7-9
____29. Daniel 10-12
____30. Esther 1-3

November

____1. Luka 14-17
____2. Luka 18-21
____3. Luka 22-24
____4. Yohane 1-3

____14. Malaki 1-4
____15. Mateyu 1-4
____16. Mateyu 5-7
____17. Mateyu 8-11
____18. Mateyu 12-15
____19. Mateyu 16-19
____20. Mateyu 20-22
____21. Mateyu 23-25
____22. Mateyu 26-28
____23. Marko 1-3
____24. Marko 4-6
____25. Marko 7-10
____26. Marko 11-13
____27. Marko 14-16
____28. Luka 1-3
____29. Luka 4-6
____30. Luka 7-9
____31. Luka 10-13

December

____1. Aroma 5-8
____2. Aroma 9-11
____3. Aroma 12-16
____4. Machitidwe 20:3-22

| | | | |
|----------|--------------------------|----------|--|
| _____5. | Yohane 4-6 | _____5. | Machitidwe 23-25 |
| _____6. | Yohane 7-10 | _____6. | Machitidwe 26-28 |
| _____7. | Yohane 11-13 | _____7. | Aefeso 1-3 |
| _____8. | Yohane 14-17 | _____8. | Aefeso 4-6 |
| _____9. | Yohane 18-21 | _____9. | Afilipi 1-4 |
| _____10. | Machitidwe 1-2 | _____10. | Akolose 1-4 |
| _____11. | Machitidwe 3-5 | _____11. | Ahebri 1-4 |
| _____12. | Machitidwe 6-9 | _____12. | Ahebri 5-7 |
| _____13. | Machitidwe 10-12 | _____13. | Ahebri 8-10 |
| _____14. | Machitidwe 13-14 | _____14. | Ahebri 11-13 |
| _____15. | Yakobo 1-2 | _____15. | Filimoni/I Petro 1-2 |
| _____16. | Yakobo 3-5 | _____16. | I Petro 3-5 |
| _____17. | Agalatiya 1-3 | _____17. | II Petro 1-3 |
| _____18. | Agalatiya 4-6 | _____18. | I Timoteyo 1-3 |
| _____19. | Machitidwe 15-18:11 | _____19. | I Timoteyo 4-6 |
| _____20. | I Atesalonika 1-5 | _____20. | Tito 1-3 |
| _____21. | II Atesalonika 1-3 | _____21. | II Timoteyo 1-4 |
| _____22. | I Akorinto 1-4 | _____22. | I Yohane 1-2; Machitidwe 18:12-19:10 |
| _____23. | I Yohane 3-5 | _____23. | I Akorinto 5-8 |
| _____24. | II Yohane, III Yohane | _____24. | I Akorinto 9-12 |
| _____25. | Chibvumbulutso 1-3, Yuda | _____25. | I Akorinto 13-16 |
| _____26. | Chibvumbulutso 4-6 | _____26. | Machitidwe 19:11-20:1; II Akorinto 1-3 |
| _____27. | Chibvumbulutso 7-9 | _____27. | II Akorinto 4-6 |
| _____28. | Chibvumbulutso 10-12 | _____28. | II Akorinto 7-9 |

- ____29. Chibvumbulutso 13-15 ____29.
____30. Chibvumbulutso 16-18 ____30.
____31. Chibvumbulutso 19-22

II Akorinto 10-13

Machitidwe 20:2/Aroma 1-4

KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

- Onaninso kafotokozeredwe ka bukhu lirilonse komwe kaperekedwa mu chaputala chino.
- Lembani dzina la bukhu lirilonse la Baibulo m'musimu.
- Pambali pake lembani mau awiri kapena atatu oumba nkota wa bukhu lonse.
- Awiriwo aperekedwa ngati chitsanzo choti muonere.
- (Pakulemba zinthu mwachidule chotere, zikuthandizirani kudziwa chithunzithunzi cha zomwe ziri m'bukhu limenelo).

Dzina la Bukhu

Zomwe Zirimo Wachidule

Genesisi

Bukhu la Chiyambi

Eksodo

Kutuluka ku Aigupto

GAWO 2: KUKONZEKERA KUSANTHULA

CHAPUTALA 3

MUSANAYAMBE

ZOLINGA:

Mukamaliza chaputala chino mukhala mukutha kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kudziwa zofunikira pakusanthula Baibulo kwabwino
- Kudziwa njira ziwiri zimene Mulungu anapereka zosanthulira Mau ake.
- Kudzindikira utumiki wophunzitsa wa Mzimu Woyera
- Kufotokoza kusiyana kwa pakati pa mkaka ndi nyama pa Mau a Mulungu
- Kudziwa makweleru atatu kuchokera pa mkaka kukafika pa nyama ya Mau a Mulungu
- Kulemba masitepe atatu kuchokera pa mkaka wa Mau kufikira pa nyama ya Mau.
- Kulemba njira zitatu za kasanthulidwe ka Mau.

VESI LOTSOGOLERA

Iye wocokera kwa Mulungu amva zonena za Mulungu; inu simumva cifukwa cakuti simuli a kwa Mulungu, (Yohane 8:47)

MAU OYAMBA

Anthu ambiri amayesera kuyamba kusanthula Baibulo ngati bukhu wamba. Amatenga Baibulo, kulitsegula, nayamba kuwerenga. Nthawi zambiri kusanthula kwao sikupita patali. Amavutika kwambiri kuti amvetse zomwe akuwerengazo. Amakanika kupeza momwe Baibulo lingagwilire ntchito m'moyo wao wa tsiku ndi tsiku; ndipo amaona kuti bukhu lotopetsa kuwerenga. Baibulo limafotokoza kuti si wina aliyense amene angathe kumvetsa bwino Mau a Mulungu. Anthu amakanika kumvetsa Mau a Mulungu chifukwa chakuti moyo wao wa uzimu sunakonzekeretsedwe kutero.

Baibulo liri ngati khomo lolowera pa maso pa Mulungu. Kuseri kwa khomo limeneli kuli chuma chazimu chodabwitsa koposa. Koma mukuyenera kukhala ndi mfungulo kuti muthe kutsegula

khomoli, apo ayi ndiye kuti simutha kulowa ndi kupeza chumachi. Baibulo limabvumbulutsa momwe tingamvetsere Mau a Mulungu. Limapereka mfungulo za momwe tingatsegulire khomo la kumvetsa zinthu zauzimu.

ZOFUNIKA PA KASANTHULIDWE KA BAIBULO

Baibulo ndi Mau a Mulungu. ndi losiyana ndi mabuku ena ndipo simungaliwerenge ngati buku wamba. Pali zinthu zina zomwe muyenera kuchita kaye musanayambe kulisanthula kuti muthe kulimvetsa bwino zinthu zakuya zauzimu za Mulungu.

Kuti mulimvetse Baibulo mukuyenera kumdziwa yemwe analemba. Yesu anati:

Iye wocokera kwa Mulungu amva zonena za Mulungu; inu simumva cifukwa cakuti simuli a kwa Mulungu, (Yohane 8:47)

Simungathe kumvetsa Mau a Mulungu popanda kumdziwa Mulunguyo. Kodi mungamdziwe bwanji Mulungu? Yesu anamuza Nikodemo, yemwe anali mtsogoleri mkulu wa chipembedzo cha Chiyuda:

Yesu anayankha nati kwa iye, Indetu, indetu, ndinena ndi iwe, Ngati munthu sabadwa mwatsopano, sakhoza kuona Ufumu wa Mulungu. (Yohane 3:3).

Munthu atha kukhala wophunzira bwino, wa chikhalidwe chabwino, komanso mwina wopembedza, koma osatha kumvetsa bwino Mau a Mulungu kufikira maso ake auzimu atatsegulidwa pa kubadwa mwatsopano.

Nikodemo anamfunsa Yesu, “Kodi izi zingatheke bwanji?” Iye sanathe kumvetsa bwino zomwe Yesu amatanthauza. Yesu anamuyankha nati:

Yesu anayankha nati kwa iye, Kodi uli mphunzitsi wa Israyeli, ndipo sudziwa izi? (Yohane 3:10)

Nikodemo anali mkulu wa chipembedzo wa Israel, koma samadziwa za kutembenuka mtima. Ndipo anafunsa...

Nikodemoananena kwa iye, Munthu akhoza bwanji kubadwa atakalamba? Kodi akhoza kulowanso m'mimba ya amace ndi kubadwa? (Yohane 3:4)

Yesu anamfotokozera kuti kubadwa mwatsopano komwe akunena kunali kwauzimu. Ndipo kumachitika kudzera nkukhulupirira mwa Yesu. Mukuyenera kuvomereza kuti ndinu wochimwa.

Mukuyenera kukhulupirira kuti Yesu anafera zochimwa zanu, mupemphe chikhululukiro cha machimo anu, ndi kumulandira Iye ngati Mpulumutsi wanu.

Munthu amene sanabadwe mwatsopano sangalandire choonadi cha Mau a Mulungu:

**Koma munthu wa cibadwidwe ca umunthu salandira za Mzimu wa Mulungu:
pakuti aziyesa zopusa; ndipo sakhoza kuzizindikira, cifukwa ziyesedwa mwauzimu.
(1 Akorinto 2:14)**

Munthu wosapulumutsidwa atha kuyamikira luso la kalembedwe ka Baibulo ndi ubwino wake. Atha kuliwerenga ngati mbiri komanso kuona malo omwe zinthuzo zidachitikira. Koma zoonadi zauzimu za Mau a Mulungu zikhalabe zobisika kwa iye pokha-pokha atalandira chikhululukiro cha machimo ake:

Pakuti mau a mtanda ali ndithu cinthu copusa kwa iwo akutayika, koma kwa ife amene tirikupulumutsidwa ali mphamvu ya Mulungu. (1 Akorinto 1:18).

ZAULERE ZA MULUNGU

Kuchokera mu nthawi imene mulandire Yesu ndi kubadwa mwatsopano, maganizo anu adzayamba kumvetsa zoonadi za Mau a Mulungu. Mwana akabadwa mthupi amasowekera chakudya, chimodzi modzinso munthu akabadwa mwatsopano amasowekera chakudya chauzimu. Chakudya chauzimuchi ndi Mau a Mulungu. Pali njira ziwiri zimene Mulungu wapereka zokuthandizani kusanthula Mau ake:

APHUNZITSI:

Mulungu amasankha okhulupirira ena kuti akhale atsogoleri mu mpingo. Ndipo ena mwa iwo ndi aphunzitsi a Mau a Mulungu:

Ndipotu Mulunguanailea ena m'Eklesia, poyamba arumwi, aciwiri aneneri, acitatu aphunzitsi, pamenepo zozizwa, pomwepo mphatso zamaciritso, mathandizo, maweruziro, malilime a mitundu mitundu. (1 Akorinto 12:28)

Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi; ndi enaaneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi; kuti akonzere oyera mtima: ku nchito ya utumiki,

kumangirira thupi la Kristu; kufikira ife tonse tikafikira ku umodzi wa cikhulupiriro, ndi wa cizindikiritso ca Mwana wa Mulungu, kwa munthu wangwiro, ku muyeso wa msinkhu wa cidzaloca Kristu. (Aefeso 4:11-13)

Mulungu amatipatsa aphunzitsi kuti azifotokozerana Mau ake momveka bwino ndi kutitsogolera kukula m'moyo wauzimu.

MPHUNZITSI WA PADERA

Mulungu waperekanso njira yachiwiri kuti inu muphunzire Mau ake. Akukulamulirani kuti muzisanthula Mau panokha.

Pakuti ife ndife pfungo labwino la Kristu, kwa Mulungu, mwa iwo akupulumutsidwa, ndi mwa iwo akuonongeka; kwa ena pfungo la imfa kuimfa;(2 Timoteyo 2:15)

Mulungu wapereka Mphunzitsi wa padera kuti akuthandizeni kusanthula Mau ake. Pamene Yesu anali padziko lapansi, anaphunzitsa anthu za choonadi cha Mulungu. Koma Iye anadziwa kuti kumapeto a imfa ndi chiukitso chake abwela kumwamba ndipo anauza ophunzira ake kuti Mphunzitsi wapadera adzatumizidwa kuti awathandize kumvetsa Mau a Mulungu. Mphunzitsi ameneyu ndi Mzimu Woyera:

Nkhosweyo, Mzimu Woyera, amene Atate adzamtuma m'dzina langa, 3 Iyeyo adzaphunzitsa Inu zonse, nadzakumbutsa inu zinthu zonse zimene ndinanena kwa inu. (Yohane 14:26)

Koma atadza Iyeyo, Mzimu wa coonadi, adzatsogolera inu m'coonadi conse; pakuti sadzalankhula za iye mwini; koma zinthu ziri zonse adzazimva, adzazilankhula; ndipo zinthu zirinkudza adzakulalikirani. (Yohane 16:13)

Nkhani ya kubwera kwa Mzimu Woyera yalembedwa pa Machitidwe a Atumwi 2. Werengani nkhanayi. Mulungu akufuna kuti nanunso mulandire kudzadzidwa kotere kwa Mzimu Woyera. Kudzera mwa Mzimu Woyera mumalandira kuthekera kwapadera kotha kumvetsa Mau a Mulungu:

Ndipo inu, kudzoza kumene munalandira kucokera kwa iye, kukhala mwa inu, ndipo simusowa kuti wina akuphunzitseni; koma 9 monga kudzoza kwace

kukuphunzitsani za zinthu zonse, ndipo kuli koona, sikuli bodza ai, ndipo monga kudaphunzitsa inu, mukhale mwa iye. (1 Yohane 2:27)

Mzimu Woyera ndi mphamvu yolenga. Ndi Mzimu wa Mulungu womwe unapumira mwa munthu mpweya wa moyo (Genesesi 2:7). Ndi Mzimu womwewo womwe unaukitsa Yesu kwa akufa (Aroma 8:11). Ndi mphamvu yolenga yomweyo ya Mzimu Woyera yomwe imapanga kuwerenga Mau a Mulungu kukhala kasanthulidwe ka luso ka Mau a Mulungu.

Tinanena koyambilira kwa phunziro lino kuti kuchita zinthu mwa luso ndiko kupanga chinthu china chatsopano. Kuphunzitsa kwa Mzimu Woyera kumapanga kuyenda kwatsopano kwa kumvetsa kwauzimu. Mzimu Woyera amapanga Baibulo kukhala latsopano, lanthete, ndi lofunikira m'moyo wanu.

MAU A MULUNGU: MKAKA NDI NYAMA

Pali milingo iwiri ya kuya kwa uzimu m'Mau a Mulungu. Mlingo wa mkaka ndi mlingo wa nyama. "Mkaka" wa Mau a Mulungu ndi zoonadi zosavuta kumvetsetseka kuti ngakhale mwana wamng'ono atha kuzimvetsa. Mwachitsanzo, dongosolo la chipulumutso. "Nyama" ya Mau a Mulungu ndi zoonadi zauzimu zakuya zomwe ndizovuta kumvetsa.

Anthu ena analandira Yesu monga Mpulumutsi wawo ndipo anadzadzidwa ndi Mzimu Woyera, koma sakukulabe mkumvetsa kwawo kwa Mau a Mulungu. Akuyamwabe mkaka wa Mau a Mulungu.

Kuthupi, palibe cholakwika kwa mwana wa Khanda kupatsidwa mkaka. Chimodzimodzinso kuuzimu. Ukabadwa kumene mwatsopano umayenera kufunafuna mkaka wa Mau a Mulungu:

lirani monga makanda alero mkaka woyenera, wopanda cinyengo, kuti mukakule nao kufikira cipulumutso; (1 Petro 2:2).

Koma imadzafika nthawi yoti mwana uja ayambe kudya chakudya cholimbirako, kuti akule bwino mthupi. Izi ziri chomwechonso muuzimu. Imafika nthawi yoti munthu achoke pa mkaka wa Mau kupita ku nyama ya Mau:

Pakuti yense wakudya mkaka alibe cizolowezi ca mau a cilungamo; pakuti ali khanda. (Ahebri 5:13-14)

Paulo ananena kuti itafika nthawi yoti okhulupirira achoke pa mkaka wa Mau kupita ku nyama, ena sanali okonzeka:

Pakuti mungakhale mwayenera kukhala aphunzitsi cifukwa ca nyengoyi, muli nako kusowanso kuti wina aphunzitse inu zoyamba za ciyambidwe ca maneno a Mulungu; ndipo mukhala onga ofuna mkaka, osati cakudya cotafuna. (Ahebri 5:12)

Kodi izi zinali chomwechi chifukwa cha chiyani? Chifukwa chiyani okhulupirira ena amafikira kwakuya kwa Mau a Mulungu pamene ena amakhala kuti akungoyandama pamwambamwamba mu mukamvetsedwe kawo ka Mau a Mulungu? Chifukwa chiyani anthu ena amakhala ndi njala ya zakuya za Mau a Mulungu koma osazipeza? Paulo analemba:

Ndipo ine, abale, sindinakhoza kulankhula ndi inu manga ndi auzimu, koma monga athupi, monga makanda mwa Kristu. Ndinaiyetsa inu mkaka, si cakudya colimba ai; pakuti simunaekhoza; ngakhale tsopano lino simucikhoza; pakuti mulinso athupi; pakuti, pokhala pali nkhwidzi ndi ndeu pakati pa inu simuli athupi kodi, ndi kuyendayenda monga mwa munthu? (1 Akorinto 3:1-3).

Samasuntha kuchoka pa mkaka wa Mau kufikira ku nyama ya Mau popeza kuti anali adakali ndi maganizo a chikunja. Kutanthauza kuti anali makanda muuzimu. Anali ndi nsanje, magawano, mkwiyo ndi machimo ena ambiri. Mkhristu akakhala ndi maganizo a chikunja, sangathe kumvetsa bwino zakuya za Mau a Mulungu. Amakhala akudalirabe pa mkaka kufikira atalapa kapena kukula mokwanira muuzimu kuti atha kudya nyama.

Ndi chikhumbokhumbo cha Mulungu kuti muchoke pa mkaka wa Mau kufikira ku nyama ya Mau. Umu ndi mmene mumaonjezerera chidziwitso chanu:

Kodi Mulungu adzaphunzitsa yani nzeru? Kodi Iye adzamvetsa yani uthengawo? iwo amene aletsedwa kuyamwa, nacotsedwa pamabere? (Yesaya 28:9).

Ndi zofunika kuti musunthe kuchoka pa mkaka kufikira ku nyama popeza kuti Mulungu amakhuthula Mzimu wake pa iwo okhwima muuzimu:

Kodi Mulungu adzaphunzitsa yani nzeru? Kodi Iye adzamvetsa yani uthengawo? iwo amene aletsedwa kuyamwa, nacotsedwa pamabere? Pakuti pali langizo ndi langizo, langizo ndi langizo; lamulo ndi lamulo, lamulo ndi lamulo; kuno pang'ono, uko pang'ono. Iai, koma ndi anthu a milomo yacilendo, ndi a lilume lina, Iye

adzalankhula kwa anthu awa; amene ananena nao, Uku ndi kupuma, mupumitsa wolema, ndi apa ndi potsitsimutsa, koma iwo anakana kumva. (Yesaya: 28:9-12)

Mulungu ankafuna kudalitsa anthu ake ndi chidzalo cha Mzimu Woyera. Ankafuna kuwatsitsimutsa ndi kuwapatsa mpumulo wauzimu, koma sanalowe chifukwa sanamve Mau ake. Anakanika kusuntha kuti afike pa nyama yauzimu popeza anali adakali pa mkaka.

KUCHOKA PA MKAKA KUFIKA PA NYAMA

Ndiyeno funso ndi lakuti, “Kodi munthu wobadwa kumene mwa Ambuye angasunthe bwanji kuchoka pa mkaka wa Mau kuti afike ku nyama ya Mau?”

lirani monga makanda alero mkaka woyenera, wopanda cinyengo, kuti mukakule nao kufikira cipulumutso; (1 Petro 2:2).

Ndi zosatheka kungofikira pa nyama. Mukuyenera kulilira komanso kukwanitsa kugaya mkaka wauzimu.

KHALANI WOMVERA MAU A MULUNGU

Iyi ndi sitepe yoyamba yofunikira. Akhristu ambiri okhala ndi maganizo a chikudya, satha kumvera zomwe aphunzira mu mkaka wa Mau a Mulungu. Mukuyenera kukhala womvera. Mukuyenera kukhala “wochita” Mau osati “wongomva” chabe:

Khalani akucita mau, osati akumva okha, ndi kudziyenga nokha. (Yakobo 1:22).

Kukula mkamvetsedwe ka Mau amabwera pamene munthu alingalira pa Mau a Mulungu ndi kumvera. Umu ndi momwe timasunthira kuchoka pa mkaka kufika pa nyama. Davide analemba kuti:

Gawo la Masalimo 119:99-104)

Popeza kuti anasunga malemba a Mulungu nawachita, kumvetsa kwake kunachuruka. Mulungu sangakutengereni ku mabvumbulutso akuya ngati simuchita zomwe mwaphun zira mu mkaka wa Mau.

FUNAFUNANI NYAMA

Kutafuna nyama kumafuna mphamvu zambiri poyerekeza ndi kumwa mkaka. Izi ziri chimodzimodzinsu muuzimu. Kupeza nyama ya Mau a Mulungu kumafunanso mphamvu zauzimu zochuluka kuposa kupeza mkaka.

Miyambo chaputala 2 akufotokoza za kafufuzidwe ka nyama:

Mwananga, ukalandira mau anga, Ndi kusunga malamulo anga; Kucherera makutu ako kunzeru, Kulozetsa mtima wako kukuzindikira; Ukaitananso luntha, Ndi kupfuulira kuti ukazindikire; Ukaifunafuna ngati siliva, Ndi kuipwaira ngati cuma cobisika; Pompo udzazindikira kuopa Yehova Ndi kumdziwadi Mulungu. (Miyambo 2:1-5).

Izi ndi njira zopezera ndi kumvetsa chidziwitso cha Mau a Mulungu:

1. Landira Mau anga: Mukhale wophunzitsika.
2. Bisa Mau anga mwa iwe: mukuyenera kuwalandira Mau ndikuwapanga kukhala mbali imodzi ya moyo ndi mzimu wanu. Musayesere kusintha Mau a Mulungu kuti agwirizane ndi momwe mufunira.
3. Tcherani khutu ku Mau a Nzeru: Mvetserani zomwe Mulungu akulankhula kwa inu kudzera m’Mau ake. Izi zikutanthauza kusintha m’makhalidwe.
4. Perekani mtima wanu kukumvetsa: Dziperekeni nokha kukumvetsa (kutanthauzira) Mau.
5. Funani nzeru ngati siliva kapena chuma chobisika: munthu atakuuzani kuti m’ munda mwanu muli kanthu ka mtengo wapatali, mungatani? Muyamba kukumba. Muchita izi pang’ono pang’ono kufikira mutachipeza. Musiya zonse zomwe mukuchita mpaka mutachita zimenezi.

Mukapanga Mau a Mulungu kukhala ofunika kwambiri pa moyo wanu ndi kuyamba kufunafuna nzeru zake mosamalitsa, mudzapeza. Koma zikuyenera kukhala poyambilira m’ moyo wanu. Muchite izi mwa nsangala ndi modzipereka monga momwe mungachitire pofunafuna chuma.

Mukatsata zimenezi pakufunafuna nyama ya Mau a Mulungu, zotsatira zake nazi:

1. Ndipo mudzadziwa kuopa Mulungu: Vesi 5
2. Ndikupeza chidziwitso cha Mulungu: Vesi 5

3. Ndipo mudzadziwa chilungamo, chiweruzo ndi chifananizo; inde njira iriyonse yabwino.
Vesi 9
4. Zikhala zokoma ku moyo wanu: (Mupeza kukhutira) Vesi 10.
5. Nzeru idzakusungani: Vesi 11
6. Kudziwa kudzakusungani: Vesi 11
7. Mudzapulumutsidwa ku zoipa zonse: Vesi 12

MAGANIZO ENA PA KASANTHULIDWE KA MAU

Awa ndi maganizo ena apadera a momwe mungasanthulire Mau.

IKANI NTHAWI YAPADERA

Ikani nthawi yapadera pa tsiku ya kusanthula Mau. Nthawiyi itengera monga mwa kukonda kwanu. Ena amakonda kupatula nthawi ya kusanthula Mau m’mapanda kucha akadali a mphamvu. Pamene ena amakonda madzulo kwambiri aliyense atakagona. Nthawi ina iriyonse yomwe mungasankhe, onesetsani kuti ndi yokhazikika kuti mukhale mukuyanjana ndi Mulungu kudzera m’Mau ake.

SANKHANI MALO A PADERA

Sankhani malo omwe ndi opanda phokoso ndi zosokoneza zina. Pakhale kuwala kokwanira koti mutha kumawerenga mosavuta. Ngati zingatheke, akhale malo oti mutha kusiya zipangizo zanu pomwepo (Baibulo, cholemba ndi polemba ndi mabuku) kuti musamavutike kutolera nthawi zonse mukazifuna.

YAMBANI MWA NJIRA YAPADERADERA.

Yambani nthawi zonse ndi pemphero. Mpempheni Mulungu atsegule nzeru zanu kuti kukathe kulandira Mau ake. Davide anati:

Kupfuula kwanga kuyandikire pamaso pano, Yehova; Mundizindikiritse monga mwa mau anu. (Masalimo 119:169)

KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

1. Werengani I Akorinto 3:1-3. Tchulani mau atatu amene Paulo akugwiritsa ntchito pofuna kufotokozerera akhristu akuthupi.

2. Kuchokera pa Miyambo 2:1-5, tchulani ma stepe 5 amene mungatsate pofufuza nyama ya amau a Mulungu.

3. Werengani Miyambo 2:5-12 ndipo tchulani zotsatira zisanu ndi ziwiri zogwiritsa ntchito zimene mwapeza posanthula mau a Mulungu.

CHAPUTALA 4

MFUNDO ZA KATANTHAUZIRIDWE KA BAIBULO

ZOLINGA

Mukamaliza phunziro lino mutha kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera.
- Kufotokozera tanthauzo la mau oti “wolunjika nawo bwino” Mau a choonadi.
- Kulemba malamulo asanu ndi limodzi a katanthauziridwe ka Baibulo
- Kupereka tanthauzo la lamulo lirilonse mwa malamulo asanu ndi limodziwa.
- Kupereka tanthauzo la mau oti kuuziridwa kwa mau olankhulidwa ndi kwatunthu.

VESI LOTSOGOLERA

Pakuti ife ndife pfungo labwino la Kristu, kwa Mulungu, mwa iwo akupulumutsidwa, ndi mwa iwo akuonongeka; kwa ena pfungo la imfa kuimfa: (2 Timoteyo 2:15)

Werenganinso vesi lotsogoleralo. “Wolunjika nawo bwino” ndi mau omwe atengedwa kuchokera ku nsembe za m’Chipangano Chakale ndipo amatanthauza “kudula molunjika.” Mu Chipangano Chakale, munthu akabweretsa nsembe ya uchimo, nyamayo imagawidwa magawo atatu. Gawo loyamba limaperekedwa kwa Mulungu. Gawo lina limaperekedwa kwa yemwe wabweretsa nsembeyo. Ndipo gawo lachitatu limapita kwa wansembe. Apa ndi pomwe panachokera mau oti “wolunjika nawo bwino.” Ndipo amatanthauza “kupereka kwa yense choyenera kupita kwa iye.”

Pakusanthula Mau nkofunika kugawa bwino Mau a Mulungu. Kutanthauza kuti mukuyenera kumvetsa chomwe chalankhulidwa ndipo kwa ndani. Komanso kutanthauzira ndi kugwiritsa bwino ntchito zomwe mwapezazo.

Pali magulu atatu komwe Mau a Mulungu amapita. Izi zalembedwa mu 1 Akorinto 10:32:

Khalani osakhumudwitsa, kapena Ayuda, kapena Ahelene, kapena Mpingo wa Mulungu; (1 Akorinto 10:32)

Malemba onse anaperekedwa kwa ife, koma si onse omwe amapita kwa ife. Mwachitsanzo, Mulungu anauza Noah kuti amange chingalawa. Nkhaniyi yalembedwa kuti tiphunzire zinthu zauzimu koma osati timange chingalawa. Gawo lina la Baibulo ndi la kwa Ayuda ndipo gawo lina ndi la kwa Amitundu (mitundu yonse yomwe si ya Chiyuda). Koma gawo lina ndi la ku Mpingo (onse okhulupirira mwa Yesu zenizeni).

Kuti mupeze tanthauzo leni leni m’Baibulo, mukuyenera kuphunzira kuligawa moyenera. Mu njira ina mutanthauzire moyenera; kupeza tanthauzo loyenera la ndimeyo. Mukuyenera kuphunzira ndi kudziwa momwe mungapezere tanthauzo leni leni la ndime yomwe mukuwerenga m’Baibulo. Yesu anadzudzula Alembi ndi Afarisi mu nthawi yake:

Koma Yesu anayankha, nati kwa iwo, Mungolakwa a osadziwa malembo, kapena mphamvu za Mulungu. (Mateyu 22:29)

Anthu amaphonya pa Malemba chifukwa chosadziwa Mau a Mulungu. Pali mfundo zomwe munthu ayenera kutsatira kuti mutanthauzire Baibulo moyenera. Pali malamulo asanu ndi limodzi omwe angakuthandizeni kutanthauzira Baibulo kuti “mugawe bwino” Mau a Mulungu.

LAMULO LA ULAMULIRO WA UMULUNGU

Lamulo ili limatanthauza kulandira Baibulo monga ulamuliro womaliza. Timakhulupirira kuti Baibulo lonse linauziridwa ndi Mulungu, kuchokera ku Genesesi mpaka Chibvumbulutso:

Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa ciphunzitso, citsutsano, cikonzero, cilangizo ca m'cilungamo: (2 Timoteyo 3:16)

Ndipo tiri nao mau a cinenero okhazikika koposa; amene mucita bwino powasamalira, monga nyali younikira m'malo a mdima, kufikira kukaca, nikauka nthanda pa mtima yanu; ndi kudziwa ici poyamba, kuti palibe cinenero ca lembo citanthauzidwa pa cokha, pakuti kale lonse cinenero sicinadza ndi cifuniro ca munthu; koma anthu a Mulungu, ogwidwa ndi Mzimu Woyera, analankhula. (2 Petro 1:19-21)

Pa mitundu iwiri ya kuuziridwa: kwa mau ndi kwatunthu.

Tikati kuuziridwa kwa mau tikutanthauza kuti liu lirilonse a m’zolembedwa zoyambirira anauziridwa ndi Mulungu. Tikati kuuziridwa kwatunthu kwa Malemba tikutanthauza kuti gawo

liri lonse la Baibulo ndilouziridwa ndi Mulungu osati magawo owerengeka okha monga anthu ena amanenera.

Tikalandira lamulo la ulamuliro waumulungu, tiona kuti palibe kutsutsana kwa Baibulo, mbiri kapena nzeru (sayansi). Ngati pali kusemphana kwina kwake ndi chifukwa chakuti mwina:

- a. Talephera kumvetsa nzeruyo (sayansi) kapena mbiri kapena mwina
- b. Nzeru yomwe tikugwiritsa ntchito leroyo siilondola. Ngati pali kusemphana, Baibulo limathetsa mlandu umenewo popeza ndi Mau ouziridwa ndi Mulungu omwe ali ndi ulamuliro wotsiriza. M'mbuyomu, pakakhala kusemphana pakati pa Baibulo ndi mbiri kapena nzeru ya sayansi anthu amachita kafukufuku ndipo mapeto ake amapeza kuti Baibulo ndi loona.

LAMULO LA KUTANTHAUZIRA ZOMWE ZALEMBEDWA

Kutanthauzira Baibulo ndiye kuti kukhulupirira zomwe zalembedwazo. Nthawi zonse tanthauzirani zomwe zalembedwazo pokhapokha ndime yomwe vesi liri ingaonetse kuti patha kukhala kuchitira mwina. Baibulo likanena kuti ana a Israel anaoloka Mtsinje wa Yordano pouma, zilandireni kuti ndi zomwe zinachitikadi. Ngati Baibulo likukamba za kugwa kwa Yeriko, zilandireni monga momwe zalembedwera m'Malemba ndi Mzimu Woyera.

Baibulo liri ndi “zithunzithunzi.” Anthu ena, kaya malo, zochitika zina pamene zikutengedwa monga momwe ziliri, zithanso kuimilira chinthu china chomwe chidzachitika mtsogolo. Chaputala 21 chitithandiza kumvetsa bwino zimenezi.

M'Baibulo mumapezekanso zizindikiro. Chizindikiro chimaimilira tanthauzo lina kuposa lodziwika kale. Mwachitsanzo, pa Marko 14:22 vinyo akugwiritsidwa ntchito ngati chizindikiro choimilira mwanzi wa Yesu Khristu. (Samamwa mwanzi weni weni). Zizindikiro zimagwiritsidwa ntchito kwambiri mu mauneneri a m'Baibulo. Mwachitsanzo, chifano chachikulu chomwe Nebukadinezara anachilota mu Daniel chinali chizindikiro cha china chake chofunika kwambiri. Gawo liri lonse la chifanochi chimaimilira ufumu womwe udzakhalepo mtsogolo (Daniel 2). Baibulo limafotokozerana chizindikiro pamene chagwiritsidwa ntchito. Mwachitsanzo, kutanthauziridwa kwa chifano chija ndi Daniel kuli pa Daniel 2:31-45.

Yesu amagwiritsa ntchito kwambiri mafanizo pophunzitsa. Fanizo ndi nkhani yomwe imaperekedwa ndi cholinga chofuna kufotokozera momveka bwino choonadi chazimu china chake. Yesu akanena fanizo limaikidwa monga fanizo koma ngati sanaonetsere kuti ndi fanizo ndiye kuti nkhaniyo itengedwe monga momwe iliri.

LAMULO LOGANIZIRA ZOMWE ZAZUNGULIRA NKHANIYO

Vesi iriyonse ya m’Baibulo ikuyenera kusanthulidwa molingana ndi zomwe zaizungulira vesiyu. Kutanthauza kuti tiyamba kuona zomwe zakambidwa m’mavesi omwe ali m’mbuyo mwake komanso omwe ali kutsogolo kwake komanso chiphunzitso chonse cha Baibulo. Ziphunzitso zambiri zonyenga zayambika pongomatula pokhapo pomwe munthu akufuna osaona nkhani yomwe ili mu ndime yonseyo kapena zomwe Baibulo limaphunzitsa.

Mwachitsanzo, Baibulo limanena kuti kulibe Mulungu. Kodi zimenezi inu mumazidziwa? Zimappezeka pa Masalimo 14:1. Komano mukawerenga ndime yonseyo mupeza izi:

Wopusa mu mtima mwake amati kulibe Mulungu (Masalimo 14:1).

Ndimeyi ikusiyana ndi zomwe timakamba poyambapo popeza kuti taiwerenga yonse.

Mukamasanthula vesi mogwirizana ndi ndime zomwe zazungulira vesilo mudzifunse mafunso awa:

1. Kodi akulankhula kapena kulemba ndi ndani?

Ngakhale Baibulo linalembedwa ndi Mulungu koma Iye anagwiritsa ntchito anthu osiyanasiyana kulemba ndi kulankhula.

2. Kodi chikukambidwa apa ndi chiyani?

Lembani mwachidule mfundo zikuluzikulu zomwe ziri mu ndimeyi.

3. Kodi uthenga ukupita kwa ndani?

Israel? Maiko a Mitundu? Mpingo? Kapena munthu wina wake?

4. Kodi analankhula chifukwa cha chiyani?

Kodi cholinga cha ndimeyi ndi chiyani? Baibulo limafotokozera lokha zolinga za mabuku ena ndi ndime zawo:

Ndipo zizindikilo zina zambiri Yesu anazicita pamaso pa akuphunzira ace, zimene sizinalembedwa m'buku ili; koma zalembedwa izi kuti mukakhulupirire kuti Yesu ndiye Kristu Mwana wa Mulungu, ndi kuti pakukhulupira mukhale nao moyo m'dzina lace. (Yohane 20:30-31).

Komabe pali magawo ena m'Baibulo omwe cholinga chake sichinaikidwe poyera. Mukuyenera kupima ndimeyo bwino lomwe kuti mukapeze cholinga cha uthengawo.

5. Kodi chinalankhulidwa liti?

Nthawi komanso zomwe zinachitika pamene nkhaniyo imalembedwa zitha kutithandiza kumvetsa bwino tanthauzo lake. Mwachitsanzo, m'mene chisokonezo chinabuka mu mpingo wa ku Akorinto Paulo anawalembera kalata. Anauza azimayi kuti akhale chete mu mpingo. Kodi izi zimatanthauza kuti asaimbe, kupemphera, kuphunzitsa, kapena kupembedza mokweza mu Mpingo?

Kuti tipeze mayankho tikuyenera kuzama kufufuza kuti zinalankhulidwa liti, chifukwa cha chiyani, kwa ndani? Mu msonkhano wa mapemphero a Chiyuda azimayi amakhala mbali imodzi kwaokha ndipo azibambo mbali inanso. Azimayi amakonda kumafunsa mafunso azimuna awo omwe anali mbali inayo koma mapemphero ali mkati. Apa ndi pomwe Paulo anaona kuti nkofunika kuwalemba kalata:

Akazi akhale cete m'Mipingo. Pakuti vsikuloledwa kwa iwo kulankhula, Koma akhale omvera, mongansocilamulo cmena, (1 Akorinto 14:34).

Kutanthauzira lembe molingana ndi mavesi ozungulira kumathandizira kudziwa tanthauzo lake lenileni. Kumatula mavesi kutha kutipangitsa kuphonya mkamvetsedwe ka Baibulo. Nthawi zambiri matanthauzo a mavesi amapezeka mu ndime zomwe zazungulira vesilo. Chitsanzo chabwino ndi fanizo la ofesa pa Mateyu 13:1-9.

Mukapitiriza kuwerenga nkhani yonseyo mupeza tanthauzo la fanizoli mu 18-23. Ndi malo ambiri onga awa omwe Baibulo lokha limapereka tanthauzo la ndime zake.

LAMULO LA KUTCHULIDWA KOYAMBA

Lamuloli limanena kuti: Kutchulidwa koyamba kwa liu, mau, chinthu kapena chochitika m'Baibulo kumapereka chithunzithunzi cha tanthauzo lake lomwe silikhala losiyana pa kutchulidwa kwake kotsatira. Mwachitsanzo, mu Genesis 3 masamba a mtengo wa mkuyu

akutchulidwa koyamba. Apa ndi pomwe Adam anasoka masamba a mkuyu navala kubisa uchimo wake ndi umaliseche wake mwayekha. Chotero, masamba a mkuyu amalankhula za kudzilungamitsa wekha, kukana thandizo la Mulungu la chiombolo, komanso kuyesera kukhala wamngwiro pamaso pa Mulungu pawekha.

Nthawi zonse masamba amkuyu akatchulidwa tanthauzo lake limakhala limeneli. Mwachitsanzo, masamba amkuyu akutchulidwa komaliza pa Mateyu 21 ndi Marko 11 ndi 13. Apa ndi pomwe tikupeza mtengo wamkuyu wa masamba obiriwira koma wopanda zipatso. Yesu anatembelera mtengowo ndipo pomwepo unafota. Kuti timvetse bwino izi tikuyenera kukumbukira lamulo la kutchulidwa koyamba ndipo tibwereranso ku Genesesi 3. Masamba amkuyu amaimilira kukana chiombolo cha Mulungu, kudzilungamitsa ndi kuyesera kudziyeretsa wekha. Mtengowu ukuimilira Israel, mtundu wodziyesa wolungama nukana Yesu Khristu. Anamukana ngati mfumu ndipo sanalandira ndondomeko yake ya chipulumutso ku uchimo. Amayesera kudzilungamitsa wokha ndi ntchito zawo.

LAMULO LA KUBWEREZA

Baibulo lonse analiuzira Mulungu. Palibe gawo lomwe ndi losafunikira m’Baibulo. Liu liri lonse ndi louziridwa chotero ndi lofunika. Chifukwa cha izi, ngati chinthu china achibwerezabwereza m’Baibulo ndiye kuti ndi chofunika kwambiri. Zimatanthauza kuti choonadi ndi chofunika kwambiri ndipo chikuyenera kubwerezedwa.

Yohane 3 akufotokozerana bwino za lamulo lobwerezabwereza ili. Yesu akuuza Nikodemo za kufunika kobadwanso mwatsopano ndipo akubwereza katatu.

Yesu anayankha nati kwa iye, Indetu, indetu, ndinena ndi iwe, Ngati munthu sabadwa mwatsopano, sakhoza kuona Ufumu wa Mulungu. (Yohane 3:3).

Yesu anayankha, Indetu, indetu, ndinena ndi iwe, Ngati munthu sabadwa mwa madzi ndi Mzimu, sakhoza kulowa ufumu wa Mulungu. (Yohane 3:5).

Usadabwe cifukwa ndinati kwa iwe, Uyenera kubadwa mwatsopano. (Yohane 3:7).

Kumbukirani kuti pamene Baibulo likubwereza chinthu kangapo ndiye kuti Mzimu Woyera akulankhula kuti “Imani kaye ndipo muone ichi.”

LAMULO LA KUKWANIRIDWA KWA BVUMBULUTSO

Lamulo ili achita kulemba m’Baibulo.

Ndi kudziwa ici poyamba, kuti palibe cinenero ca lembo citanthauzidwa pa cokha, (2 Petro 1:20-21).

Lamulo la kukwaniridwa kwa bvumbulutso limati: Choonadi chonse cha Mau a Mulungu pa nkhani iriyonse sichikuyenera kuchotsedwa pa ndime inayake yapayokhayokha. Tikuyenera kuona kaye zonse zomwe Baibulo likukamba pa nkhani imeneyo tisanafike pa mlingo wonena kuti ili ndi tanthauzo la ndimeyi. Ichi ndi chifukwa chake lamuloli limatchedwa la “bvumbulutso lokwaniridwa.

Simukuyenera kupanga chiphunzitso kapena chikhulupiriro kuchokera pa ndime imodzi yokha ya m’Baibulo ayi. Santhulanibe kufikira tanthauzo lanulo lifanane ndi zonse zomwe Baibulo limaphunzitsa.

KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

Pali mavesi ambiri m'Baibulo omwe amatsimikizira za kuuziridwa kwa Mau a Mulungu. Onani mavesi otsatirawa ndi kulemba mwachidule zomwe akulankhula:

LEMBA

NDEMANGA

Ahebri 1:1

1 Atesalonika 2:13

2 Timoteyo 3:16

1 Akorinto 14:37

1 Akorinto 2: 7-13

1 Akorinto 11:23

Agalatiya 1:11-20

Aefeso 3:1-10

2 Petro 3:16

CHAPUTALA 5

MBIRI YA BAIBULO

ZOLINGA

Mukamaliza chaputala chino muzikwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kudziwa nthawi zofunika kwambiri mu mbiri ya Baibulo
- Kufotokozero moyo wa tsiku ndi tsiku mu nthawi ya m’Baibulo.
- Kufotokozero tanthauzo la kafukufuku wa mbiri yakale ya Baibulo.

VESI LOTSOGOLERA

**Kuyambira kale ndinadziwa mu mboni zanu, Kuti munazikhazika kosatha,
(Masalimo 119:152)**

MAU OYAMBA

Gawo liri lonse la Baibulo linachitika pa nthawi inayake pakati pa anthu a chikhalidwe chinachake. Kumvetsa bwino tanthauzo la ndime kumakhuza zinthu zimenezi. Chaputala chino chikukamba mwachidule za mbiri ya Baibulo ndi kufotokozero mwatsatanetsatane za moyo tsiku ndi tsiku wa anthu nthawi imeneyo.

MBIRI YA NTHAWI YOMWE ZINTHU ZINACHITIKIRA

Mbiri ya nthawi yomwe zinthu zinachitikira imakamba za nthawi imene chinthu china chinachitikira. Ndipo zochitikazo zimaikidwa mu dongosolo lake molingana ndi momwe zinachitikira.

Nthawi ya pansi pano inagawidwa m’magawo awiri. Ndipo m’Chingerezi magawowa amaonetsedwa ndi mau oti BC kapena AD kumapeto kwa chakacho.

BC: chaka chokhala ndi mau awa kumapeto ndiye chochitikacho chinachitika Yesu asanabadwe.

AD: chaka chokhala ndi mau awa kumapeto ndiye kuti chochitikacho chinachitika Yesu atabadwa kale.

Mwachitsanzo akalemba kuti 250 BC, zimatanthauza zaka 250 Yesu asanabadwe. Ndipo tikanena kuti chinthu chinachitika mu 700 AD ndiye kuti zaka 700 Yesu atabadwa.

Dziwani chinthu ichi: Mu BC timachotsera zaka pamene chaka chatha pamene mu AD timaonjezera chaka chikatha. Mwachitsanzo, tikachoka mu 33 BC timafika mu 32 koma mu AD tikachoka mu 33 timafika mu 34.

Pali njira zingapo zomwe timagwiritsa kuti tidziwe nthawi yeniyeniyeni yomwe chinthu chinachitikira:

1. Baibulo lokha limanena za nthawiyo.
2. Kudzera mu zolembedwa za olemba mbiri akale.
3. Kudzera mkafukufuku wa mbiri yakale yomwe imasanthula zinthu zakale kwambiri. Anthu amayesetsa kudziwa zambiri za zomwe zimachitika kale posanthula zinthu zotsala za zinthu zomwe anthuwo ankagwiritsa ntchito monga zipande, mipaliro, nyumba kapena zovala. Kafukufuku wa mbiri yakale ya Baibulo ndiko kusanthula bwino zotsalira za anthu omwe amakhala malo omwe atchulidwa m'Baibulo. Zochitika zina zinapatsidwa masiku ake anthu atasanthula zinthu zomwe anazipeza.

MBIRI YA MNDANDANDA WA BAIBULO

Mndandanda wa zochitika m'Baibulo wagawidwa m'nthawi khumi ndi ziwiri (12). Tchati chili m'musichi chikuonetsa mndandanda wa zochitika m'Baibulo. Pakati pali zochitika kuchokera nthawi ya Abraham kufikira nthawi ya Uthenga Wabwino. Kumanzere kuli mabuku a m'Chipangano Chakale ndipo kumanja kuli mabuku a m'Chipangano Chatsopano kulumikizitsa chochitika ndi mabuku omwe analembedwa mu nthawi imeneyo.

Muonenso kuti pakati pa Chipangano Chakale ndi Chatsopano pali zaka 386 ndipo kuti palibe bukhu lililonse lomwe linalembedwa. Pamene musanthula Baibulo lanu, chonde gwiritsani ntchito mndandandawu ndi wothandiza kwambiri.

Tchati 1: Tsatanetsatane wa Mbiri ya Baibulo

| | | |
|-----------|---------------------|----------|
| YOSHUA | 4. KUlowa m’Kenani | |
| OWERUZA | 5. Oweruza | |
| RUTE | | |
| | 6. Mafumu | YOBU |
| | | MASALIMO |
| | | MIYAMBO |
| | | MLALIKI |
| | | NYIMBO |
| | | SOLOMO |
| | | YA |
| I SAMUEL | | YESAYA |
| II SAMUEL | | YEREMIYA |
| | | MALIRO |
| I MAFUMU | | EZEKIEL |
| II MAFUMU | | DANIEL |
| | | HOSEYA |
| | | YOWELI |
| | | AMOSI |
| I MBIRI | 7. Maufumu awiri | OBADIYA |
| II MBIRI | 8. Yuda yekha | YONA |
| | | MIKA |
| | | NAHUM |
| | | HABAKUKU |
| EZRA | 9. Ukapolo | ZAFANIYA |
| NEHEMIYA | | HAGAYI |
| MALAKI | 10. Kubwezeretsedwa | ZEKARIYA |

MATEYU

PAKATI PA ZIPANGANO

MARKO

11. Moyo wa Khristu

LUKA

YOHANE

AROMA

I NDI II AKORINTO

AGALATIYA

AEFESO

AFILIPO

AKOLOSE

I NDI II

ATESALONIKA

MACHITIDWE

12. Kufalitsidwa kwa Uthenga

I NDI II TIMOTEYO

FILIMONI

TITO

AHEBRI

YAKOBO

I NDI II PETRO

I, II, NDI III

YOHANE

YUDA

CHIBVUMBULUTSO

Tsopano werengani tsatanetsatane wa zomwe zinachitika mu nthawi 12 za mu mbiri ya Baibulo:

1. Chilengedwe mpaka Abraham (Kuchokera pa chilengedwe mpaka 2000 BC):

Chilengedwe cha dziko, kugwa kwa munthu, kuphedwa kwa Abel ndi m' mbale wake Kaini, Noah ndi chigumula, ndi Nsanja ya Babulo ndi nkhani zikuluzikulu za nthawi imeneyi.

2. Abraham mpaka Mose (2000 mpaka 1500 BC)

Nthawiyi ikutenga zaka 500. Nkhani yaikulu mgawo limeneli ndi ya Abraham ndi mbado wake. Kuchokera mwa Abraham, Mulungu anadzutsa mtundu womwe anaugwiritsa ntchito kudzibvumbulutsa yekha ku maiko onse a dziko lapansi. Mu nthawiyi muli nkhani za Isake, mwana wa Abraham, ndi Yakobo mwana wa Isake. Ndipo nthawiyi ikufika pa chimake ndi nkhani ya Yosefe, mwana wa Yakobo, yemwe anagulitsidwa ku ukapolo wa ku Aigupto nakhala wolamulira wamkulu. Kenako Yakobo ndi banja lake anakakhala ku Aigupto kulondola Yosefe

3. Ulendo wa ku Kenani (1500 mpaka 1460 BC)

Pakati pa kumapeto kweni kweni kwa Bukhu la Genesesi ndi kumayambiro a bukhu la Eksodo panadutsa zaka pafupifupi 100. Banja la Yakobo linakula kukhala mtundu wa Israel mu nthawi imeneyi. Aigupto anayamba kukhala ndi mantha chifukwa cha kukula msanga kwa fuko la Israel ndipo anawapanga kukhala akapolo. Mose anabadwa natulutsa ana Aisrael mu Aigupto mozizwitsa. Atatha chaka chatunthu pa phiri la Sinai anazungulira mchipululu kwa zaka 38. Nthawiyi ikutsekedwa ndi imfa ya Mose ndikuti utsogoleri wa ana Aisrael ukugwa m' manja mwa Yoswa.

4. Kugonjetsa Kenani (1450-1102 BC)

Mu nthawiyi Yoswa anatsogolera Israel kulowa mu Kenani ndi kutenga dziko limene Mulungu anawalonjeza. Pamene anagonjetsa anthu oipa okhala derali powathira nkhondo, anagawa dzikolo ku mafuko khumi ndi awiri. Zonse zinatenga zaka 10 komanso zalembedwa m' bukhu la Yoswa.

5. Oweruza (1450-1102)

Iyi ndi nthawi imene Mulungu anadzutsa oweruza kuti alamulire anthu a Israel. Inali nthawi ya mdima wauzimu waukulu mu mbiri ya Israel. Nthawi ya oweruza inali zaka 348.

6. Ufumu (1102-982 BC)

Samuel ndiye woweruza womaliza wa Israel, anakhazikitsa Ufumu wa Israel ndipo anadzodza Sauli kukhala mfumu. Mafumu atatu, Sauli, Davide ndi Solomoni, analamulira kwa zaka 40 aliyense. Apa ndi pomwe Ufumu wa Israel unafika pachimake kukula mphamvu mu mbiri yonse ya Israel. Ulamuliro wa Israel unakhazikitsidwa mwa mphamvu ndipo malire anakuliziridwa. Nkhani ya nthawiyi komanso ndi nthawi zina zotsatirapo zalembedwa m'mabuku a 1 ndi 2 Samuel, 1 ndi 2 Mafumu, ndi 1 ndi 2 Mbiri. Nthawi ya Ufumu inali zaka 120.

7. Maufumu Awiri (987-722).

Pamene mwana woipa wa Mfumu Solomo, Rehoboam, analowa pa mpando, mafuko onse a Kumpoto anaukira. Anakhazikitsa ufumu wapadera wa Israel. Ufumu wa Kumwera umatchedwa Ufumu wa Yuda. Kwa zaka 259 Israel anali ndi maufumu awiri ogawika chomwechi.

8. Yuda yekha (722-587 BC)

Israel, Ufumu wa Kumpoto, analandidwa ndi Aasuri mu 722 BC. Ndipo anthu anatengedwa ukapolo kunka ku Asuri. Zitachitika izi, Ufumu wa Yuda wakumpoto unakhala zaka 135. Mafumu a ku Yuda anaonetsa kuopa Mulungu ndithu ndipo anthu ake sanazame kwambiri mu uchimo.

9. Ukapolo (587-538 BC)

Posatengera machenjezo a aneneri, Yuda ananka nalowa mu uchimo wakuya kufikira Mulungu analola Mfumu Nebukadinezara kuti awagonjetse nawatenga ukapolo kunka ku Babulo. Mzinda wa Yerusalemu unaonongedwa ndipo anthu a Mulungu, omwe nthawi inayake anaoloka mtsinje wa Yordano mozizwitsa anayendetsedwa mu nseu atamangidwa maunyolo.

10. Kubwezeretsedwa (538-391 B.C.)

Pamene mfumu yotchedwa Koresi anakhala pa mpando, analola anthu a Mulungu kuti azipita kwao kukamanga Yerusalemu ndi kachisi. Zerubabelo anatsogolera gulu limene linabwerera kukhazikika m'dziko la malonjezano. Nkhani za nthawi ziri mu mabuku a Ezra, Nehemiya ndi Estere. Nthawi yobwezeretsayi inali zaka 147.

Pakati pa zipangano (391-5 B.C.)

Chipangano Chakale chikumalizika ndi kukhazikitsidwanso kwa anthu a Mulungu, Israel, ku Kanani. Kenako panali nthawi yokwanira zaka 400 pakati pa Chipangano Chakale ndi Chatsopano. Panalibe bukhu lirilonse la m'Baibulo lomwe linalembedwa mu nthawi imeneyi kotero zochitika za nthawi imeneyi timazipeza kudzera kwa olemba mbiri wamba.

Mu nthawi imeneyi Palestina amalumulidwa ndi Aperezi (536-333 B.C.), Agiriki (333-323 B.C.), Aigupto 323-204 B.C.), Asuri 204-165 B.C.), Amakabeyo (165-63 B.C.), ndi Aroma (63 B.C. mpaka nthawi yakubadwa kwa Khristu).

11. Moyo wa Khristu (5 B.C. to 28 A.D.):

Zitatha zaka 400, Mulungu anadzutsa Yohane M'batizi kuti akonzekeretse njira ya kubwera kwa Ambuye Yesu Khristu. Yesu ndiye wopulumutsa anthu ochimwa. Lonjezo la dongosolo la chipulumutsoli linalengezedwa m'munda wa Eden pa Genesis 3:15. Yesu anabadwa mozizwitsa kudzera mwa namwali, nadzibvumbulutsa yekha kwa Israel ngati Messiya, nakanidwa, napachikidwa chifukwa cha machimo a anthu onse, naukitsidwa ndi mphamvu ya Mulungu. Mateyu, Marko, Luka ndi Yohane alemba za mbiri iyi yomwe inatenga zaka 33.

12. Kufalitsidwa kwa Uthenga Wabwino (28-100 A.D.)

Mu nthawi iyi muli nkhanu zomwe zinachitika Yesu atakwera kunka kumwamba atatha kuuka kwa akufa. Imakamba za kufalitsidwa kwa Uthenga Wabwino kuchokera ku Yerusalemu kunka ku Yudeya, Samariya, kufikira dziko lonse lapansi.

Tchati 2: Oweruza a Israel

Chipangano Chakale chili ndi nkhanu zambiri zomwe zinachitika nthawi imene Israel amalumulidwa ndi Oweruza. Iwo analumulira Israel adakalibe mafumu. Nkhani za oweruza

zalembedwa m’bukhu la Oweruza. Gwiritsani ntchito tchati ili m’musiyi muone nthawi yomwe nkhanizi zinachitikira:

| Ndime | Dzina | Zaka (B.C.) | Zaka Zonse |
|-----------------|-----------|-------------|------------|
| Oweruza 3:7-11 | Othniel | 1400-1360 | 40 |
| Oweruza 3:12-31 | Ehud | 1360-1280 | 80 |
| Oweruza 3:12-31 | Shamgar | 1280 | 1 |
| Oweruza 4-5 | Deborah | 1280-1240 | 40 |
| Oweruza 6-8:32 | Gideon | 1240 -1200 | 40 |
| Oweruza 9 | Abimelech | 1200-1197 | 3 |
| Oweruza 10:1-2 | Tola | 1197-1174 | 23 |
| Oweruza 10:3-5 | Jari | 1174-1152 | 22 |
| Oweruza 10:6-12 | Yefita | 1152-1146 | 6 |
| Oweruza 10:6-12 | Ibzan | 1146-1138 | 8 |
| Oweruza 10:6-12 | Elon | 1138-1128 | 10 |
| Oweruza 10:6-12 | Abdon | 1128-1121 | 7 |
| Oweruza 13-16 | Sampson | 1121-1101 | 20 |

Tchati 3: Mafumu a Israel ndi Yuda

Nkhani zinanso zinachitika mu nthawi ya mafumu osiyana-siyana a Israel ndi Yuda. Onani tchati iyi:

Mafumu a Israel

| Dzina | Zaka Zonse | Masiku (B.C.) Ndime |
|-------|------------|---------------------|
|-------|------------|---------------------|

| | | | |
|-------------|-----------|---------|-----------------------------------|
| Yeroboamu I | 22 | 976-954 | I Mafumu 11:26-14:20 |
| Nadabu | 2 | 954-953 | I Mafumu 15:25-28 |
| Baasha | 24 | 953-930 | I Mafumu 15:27-16:7 |
| Elah | 2 | 930-929 | I Mafumu 16:6-14 |
| Zimri | (7 days) | 929 | I Mafumu 16:9-20 |
| Omri | 12 | 929-918 | I Mafumu 16:15-28 |
| Ahab | 21 | 918-898 | I Mafumu 16:28-22:40 |
| Ahaziya | 1 | 898-897 | I Mafumu 22:40- II Mafumu 1:18 |
| Yehoram | 11 | 897-885 | II Mafumu 3:1-9:25 |
| Yehu | 28 | 885-857 | II Mafumu 9:1-10:36 |
| Yehoahaz | 16 | 857-841 | II Mafumu 13:1-9 |
| Yehoash | 16 | 841-825 | II Mafumu 13:10- 14:16 |
| Yeroboam II | 40 | 825-773 | II Mafumu 14:23-29 |
| Zekariya | ½ | 773-772 | II Mafumu 14:29- 15:12 |
| Shallum | (1 month) | 772 | II Mafumu 15:10-15 |
| Menahem | 10 | 772-762 | II Mafumu 15:14-22 |
| Pekahiya | 2 | 762-760 | II Mafumu 15:22-26 |

| | | | |
|-------|----|---------|----------------------|
| Pekah | 20 | 760-730 | II Mafumu 15:27-31 |
| Hosea | 9 | 730-721 | II Mafumu 15:30-17:6 |

Mafumu a Yuda

| Dzina | Zaka Zonse | Masiku (B.C.) Ndime | |
|-----------------|------------|---------------------|----------------------|
| Rehoboam | 17 | 976-959 | I Mafumu 11:42-14:31 |
| Abijam | 3 | 959-996 | I Mafumu 14:31-15:8 |
| Asa | 41 | 956-915 | I Mafumu 15:8-24 |
| Jehosafati | 25 | 915-893 | I Mafumu 22:41-50 |
| Johoram | 8 | 893-886 | II Mafumu 8:16-24 |
| Ahaziya | 1 | 886-885 | II Mafumu 8:24-9:29 |
| Ataliya | 6 | 885-879 | II Mafumu 11:1-20 |
| Yoasi | 40 | 879-840 | II Mafumu 11:1-12:21 |
| Amaziya | 29 | 840-811 | II Mafumu 14:1-20 |
| Azariya (Uziya) | 52 | 811-759 | II Mafumu 15:1-7 |
| Yotamu | 18 | 759-743 | II Mafumu 15:32-38 |
| Ahazi | 19 | 743-727 | II Mafumu 16:1-20 |
| Hezekiya | 29 | 727-698 | II Mafumu 18:1-20:21 |
| Manase | 55 | 698-643 | II Mafumu 21:1-18 |
| Amoni | 2 | 643-640 | II Mafumu 21:19-26 |

| | | | |
|----------|----------------|---------|-----------------------|
| Josiya | 31 | 640-609 | II Mafumu 22:1-23:30 |
| Yehoazi | (miyezi itatu) | 609 | II Mafumu 23:31-33 |
| Yehoakim | 11 | 609-597 | II Mafumu 23:34-24:5 |
| Yehoakin | (miyezi itatu) | 597 | II Mafumu 24:6-16 |
| Zedekiya | 11 | 597 | II Mafumu 24:17-25:30 |

Tchati 4: Aneneri a Chipangano Chakale

Popeza mabuku ambiri a Chipangano Chakale ndi uneneri, nkofunika kudziwa nthawi imene m'neneriyo anakhala ndi kugwira ntchito yake. Gwiritsani nthito tchati iyi kuti mudziwe:

| Dzina | Kopita Uneneri | Masiku |
|-----------------|----------------|-----------------------------|
| Yona | Asuri | Usanafike Ukapolo (800-650) |
| Nahumu | Asuri | Usanafike Ukapolo (800-650) |
| Obadiya | Edomu | Usanafike Ukapolo (800-650) |
| Hoseya | Israel | Usanafike Ukapolo (800-650) |
| Amosi | Israel | Usanafike Ukapolo (800-650) |
| Yesaya/Yeremiya | Yuda | Usanafike Ukapolo (800-650) |
| Yeremiya/Maliri | Yuda | Usanafike Ukapolo (800-650) |
| Yoel | Yuda | Usanafike Ukapolo (800-650) |
| Mika | Yuda | Usanafike Ukapolo (800-650) |
| Habukuku | Yuda | Usanafike Ukapolo (800-650) |

| | | |
|----------|------|-----------------------------|
| Zefaniya | Yuda | Usanafike Ukapolo (800-650) |
| Ezekiel | Yuda | Nthawi ya Ukapolo (606-536) |
| Daniel | Yuda | Nthawi ya Ukapolo (606-536) |
| Hagayi | Yuda | Utatha Ukapolo (536-400) |
| Zekariya | Yuda | Utatha Ukapolo (536-400) |
| Malaki | Yuda | Utatha Ukapolo (536-400) |

MOMWE ANTHU AMAKHALIRA

Baibulo, anthu olemba mbiri komanso ofufuza zinthu zakale zimafotokozerabwino momwe anthu a m’Baibulo amakhaira moyo wawo wa tsiku ndi tsiku. Isanafike nthawi yoti apite ku Aigupto, anthu a Israel amakhala m’mahema. Ankakhala akuyendayenda kufuna malo omwe angapeze nsipu ndi madzi abwino posamalira ziweto zawo.

Atatha kuchoka kwa Aigupto ndi kuchoka m’chipululu, Israel anakhazikika m’dziko la malonjezano la Kenani. Kuchokera mu nthawi imeneyo anthu anayamba kukhala moyo wokhazikika womwe sumasinthasinthanakupita kwa nthawi.

Alimi amakhala akugwira ntchito m’mindayawo kapena kupanga zinthu zaluso pamene azimayi ndi ana amasunga khomo. Ulimi wa mbeu ndi ziweto zinali ntchito zofunikira koposa.

Kumachitikanso usodzi ndi ntchito zaluso zosiyanasiyana m’ mudzi monga kupala matabwa, kuumba mbiya, ndi kufufuta zikopa.

Madzi amakhala osowa popeza nthaka imakhala yotentha ndi youma nthawi zambiri m’chaka.

Anthu amatunga madzi pa chitsime cha m’ mudzi ndi amatungira mu zidebe zopangidwa ndi zikopa zambuzi. Awa amakhala malo abwino ochezera azimayi.

Anthu amavala mikanjo yaitali yopita mphepo bwino. Nsalu za mikanjoiyimatengera kupeza bwino kwa munthu. Anthu ochita bwino amavala nsalu zokongoletsedwa ndi zowala. Nthawi zambiri zovala zimatha kuonetsa ntchito ya munthu. Mwachitsanzo, ansembe amavala mikanjo yapadera-dera ndipo alembi amavala mkanjo watundu wosiyana ndi ena onse. Nsapato zawo

zinali nkhwaira zopangidwa ndi zikopa za ng'ombe ndipo zimakhala ndi zingwe zomangira kumwendo.

Dongosolo labanja limakonzedwa popeza achinyamata samachezera limodzi nthawi zambiri. Popeza kuti namwali anali munthu wodalirika pa ntchito zapakhomo, mnyamata amayenera kulipira lobola. Moyo wawo wa tsiku ndi tsiku umadalira zochitika pakhomo.

M'Chipangano Chakale kunalibe masukulu a ana a anthu wamba. Amaphunzitsidwa maluso ambiri komanso za chipembedzo kuchokera kwa makolo awo. Mu nthawi ya Yesu, mayi anali ndi udindo waukulu wophunzitsa mtsikana pakhomo. Anyamata amayamba kupita ku sunagoge kokaphunzira akwanitsa zaka zisanu ndi chimodzi. Iwo amagwiritsa ntchito Bukhu la Chipangano Chakale pakuphunzira mbiri, chilengedwe, nzeru ndi chilamulo. Ana ochita bwino pa maphunziro amawatumiza ku Yerusalemu kukaphunzira pansu pa Rabi (mphunzitsi). Mnyamata wina aliyense amayenera kuphunzira kenakake kompezetsa thandizo m'moyo wake. Ndipo mnyamata akakwanitsa zaka khumi ndi zitatu amakhala “mwana wa chilamulo” ndiye kuti wakula.

Imfa pakati pa Ayuda imakhala ndi dongosolo lapadera lobuma. Nthawi zina amatha kulemba aganyu olira maliro. M'Chipangano Chatsopano, maliro amawadzodza ndi mafuta ndi kukulunga mu nsalu zakumanda zapadera. Anthu osauka amaikidwa m'manda wamba kapena ku mphanga, koma anthu ochita bwino amaikidwa m'manda osema mu tanthwe ndi kuika chotseka pakhomo.

Panalibe kusiyana pakati pa lamulo ladziko ndi lachipembedzo mu Israel. Pachipata cha mzinda kapena mudzi ndiye anali malo oweruzira milandu. Bwalo lalikulu mu Chipangano Chatsopano anali gulu la amuna 70 lotchedwa Sanhedrin ndipo amakumana ku kachisi. Aroma, omwe anali olamulira mu Chipangano Chatsopano, anapereka mphamvu kwa Ayuda kuti atha kupereka chigamulo chiri chonse molingana ndi chilamulo chawo kupatula chigamulo chakupha.

Moyo wa chipembedzo mu Israel unakhazikika pa chihema poyamba kenako pa kachisi ku Yerusalemu. Malamulo a chipembedzo amayendetsedwa ndi ansembe pamodzi ndi Alevi. Tsiku lalikulu kwambiri pa chaka linali tsiku lopereka nsembe ya chikhululukiro (Day of Atonement). Pa tsikuli wansembe wamkuru amalowa m'chipinda chamkati kwambiri cha kachisi kukapereka nsembe ya chikhululukiro cha machimo a iye mwini komanso machimo a anthu onse.

Zikondwerero zina zinali monga Pasaka, pamene amakumbukira kuturutsidwa kwao m’dziko la Aigupto. Chikondwerero cha Pentecost chimatsegulira kholola ndipo chikondwerero cha Mahema chinali cha kholola. Chikondwerero cha Purim chimakumbutsa kupulumutsidwa kwa Aisrael ndi Estere, ndipo chikondwerero cha malipenga chinali chikondwerero cha kulowa chaka chatsopano.

Pakati pa kumapeto kwa Chipangano Chakale ndi kumayambiro kwa Chipangano Chatsopano chipembedzo chinayamba kuchitikira m’masunagogi osati ku kachisi. Kusintha uku kunachitika kuyambira nthawi imene Israel anali ku ukapolo ndipo ku Yerusalemu kunalibe kachisi. Amuna okhaokha ndi omwe amatenga gawo pa mwambo wa mapemphero. Azimayi pamodzi ndi ana onse amakhala mbali ina yosiyana ndi komwe kumakhala azibambo. M’dongosolo la mapemphero mumakhala mau ovomereza (statement of creed), pemphero, komanso kuwerengedwa kwa chilamulo ndi aneneri. Kenako pamakhala ulaliki ndipo ukatha azibambo amafunsa mafunso wolalikirayo.

Malemba a m’Chipangano Chakale analembedwa pa chimpukutu chopatulika ndipo chimatsegulidwa ndi akadaulo pa chilamulo okha. Mwa apa ndi apo anthu amatha kupita kukapemphera ku kachisi ku Yerusalemu yemwe pa nthawiyi anali atamangidwa. Kachisiyu anali ofanana ndi yemwe Solomo adamanga m’Chipangano Chakale.

Moyo wa banja ndi wa tsiku ndi tsiku umenewu ndi pomwe nkhanzi za m’Baibulo zimatsamira ndipo sunasinthe konse kwa zaka mazanamazana. Nkhanzi zimatsamiranso pa nkondo za akalonga ozungulira Israel ndi mphamvu ya ulamuliro wa Chiroma. Mu nthawi ya Yesu, Israel anali panso pa ulamuliro wa Chiroma.

CHAPUTALA 6

KUSANJA MITU, KUIKA ZIZINDIKIRO, KUGAWA NKHANI

ZOLINGA

Pamapeto pa chaputala chino mukhala mukutha kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kugwiritsa ntchito njira yoikira zizindikiro m’Baibulo
- Kusanja mitu ya nkhani
- Kupanga tchati youmba mkota

VESI LOTSOGOLERA

Mboni zanu ndizo zolungama kosatha; Mundizindikiritse izi, ndipo ndidzakhala ndi moyo. (Masalimo 119:144).

MAU OTSOGOLERA

Pali zinthu zitatu zomwe zingakuthandizeni inu kupindula pa kusanthula kwanu kwa Baibulo. Zinthu zitatu zimenezi ndi kuika zizindikiro, kukonza mitu, ndi kukonza tchati.

KUIKA ZIZINDIKIRO (MARKING)

Kuika zizindikiro ndi njira yotsikindika pa ndime zina za m’Baibulo. Ndipo izi zimakuthandizani kupeza mosavuta mavesi pa mitu yosiyana siyana. Mutha kuchita izi podula mzere kungsi kwa mavesi omwe mwasankhawo. Ngati muli ndi cholemba makaka kapena chekeni muthanso kugwiritsa ntchito. Ngati zonsezi mulibe mutha kumangoika zizindikiro m’mbali mwa ndime yomwe mwaikonda.

Gwiritsani ntchito makaka awa poika zizindikiro mu ndime za m’Baibulo lanu.

Ofiira: Pamavesi onse omwe akukamba za chipulumutso. Kufiira kumaimilira mwanzi wa Yesu Khristu. Muthanso kugwiritsa ntchito chizindikiro cha mtanda pa mavesi a chipulumutso.

Girini: Makaka awa amaimilira zinthu zomwe zikukula. Gwiritsani ntchito makaka pa mavesi okamba za kukula m’moyo wauzimu. Muthanso kugwiritsa ntchito duwa kuimilira kukula.

Bulu: Awa ndi makaka akumwamba. Gwiritsani ntchito makaka awa pa mavesi okamba za kubweranso kwachiwiri kwa Yesu Khristu, Yerusalemu Watsopano, ndi Kumwamba. Ngati mukugwiritsa ntchito zizindikiro, lembani chizindikiro cha chisoti chaufumu pambali pa ndimeyo m’Baibulo lanu. Chisoti cha ufumuchi chikuimilira Ufumu wa Kumwamba.

Makaka otuwa (brown): Pamene mbeu zacha pokonzekera kholola zimakhala ndi makaka otuwa. Yesu anagwiritsa ntchito chitsanzo cha kholola polankhula za kuchitira umboni. Gwiritsani ntchito makaka otuwa pa ndime zonse zokamba za kuchitira umboni za Yesu. Muthanso kugwiritsa ntchito chizindikiro ichi (#) chomwe chimaimilira chiwerengero cha zinthu. Gwiritsani ntchito ichi kuti chikukumbutseni chiwerengero cha anthu omwe akuyenera kumva Uthenga Wabwino.

Mutha kusankha makaka ena owonjezera poika zizindikiro pa ndime za m’Baibulo zokamba nkhani zosiyanasiyana: makaka akuda, apinki, ngakhale yelo.

KUKONZA MLOZO

Mlozo ndi njira yosanjira mitu ya zomwe munthu akufuna kulankhula kapena kuwerenga. Ndi mlozo nkhani zimalembedwa mwachidule kuti zigwiritsidwe ntchito mu utumiki kapena pakusanthula kwa mtsogolo. Mlozo umakhala umayenera kukhala ndi mutu waukulu womwe umakhala tsinde la zomwe mukusanthula.

Mutatha kupeza mutu woti musanthule, pezani mfundo zikuluzikulu zomwe zikukamba zamutu womwe mwasankhawo. Kenako mupeza mfundo zing’onozing’ono pansi pa mfundo zikuluzikulu zomwe muli nazo.

Pali njira zambiri zokonzera mlozo. Tasankha njira imodzi yogwiritsa ntchito ma nambala poonetsa mfundo zikuluzikulu. Ndipo mfundo zing’onozing’ono zaonetsedwa ndi malembo akuluakulu. Ngati pali mfundo zina pansi pa mfundo zimenezi zionetsedwa ndi manambala ena. Onani chitsanzo chiri m’musichi chomwe chikuumba mkota za kukonza mlozo:

IKANI MUTU APA

- I. Ichi ndi chilembo choonetsa mfundo yaikulu yoyamba.
 - A. Chilembo ichi chikuonetsa mfundo yaying’ono pansi pa mfundo yaikulu yoyambayo.

1. Ngati pali mfundo yaing'ono kwambiri pansi pa mfundo yaing'ono ikhala ndi chilembo chimenechi.
 2. Mwina pali mfundo ina yaing'ono kwambiri pansi pa mfundo yaing'ono ya
 - (A). Ngati pali zina pitirizani (3), (4), mpaka mtsogolo.
 - B. Mfundo yoyamba (I) mwina itha kukhala ndi mfundo zazing'ono zina. Ngati ndi choncho muzipita pansi ndi zilembo (A, B, C, D) mpaka pamene mukathere. Onetsetsani kuti mfundo iriyonse yomwe mukulemba ikhale ikukamba za mfundo yoyamba (I) yomwe iri pamwamba penipeni.
- II. Kuti muonetse mfundo yachiwiri muika chilembo chotsatira chimenechi.
- A. Kenako mfundo zing'onozing'ono m'musimu monga momwe ziriri mu mndandanda uli pamwambawo.

Taika chitsanzo cha mlozo wandime yomwe iri pa Aroma 12:1-2.

(Aroma 12:1-2)

Mlozo wa ndime imeneyi utha kuoneka motere:

NJIRA YOPEZERA CHIFUNIRO CHA MULUNGU

- I. Perekani matupi anu nsembe yamoyo
 - A. Yoyera
 - B. Yobvomerezeka
- II. Musafanizidwe ndi dziko lapansi
 - A. Khalani wosinthika
1. Timasinthika mwa kusandulika kwa mtima wathu.
- III. Izi zitithandiza kupeza chifuniro cha Mulungu chomwe ndi:
 - A. Chabwino
 - B. Chobvomerezeka
 - C. Changwiro

Mutha kuona momwe mlozo uwu walembera mwachidule za njira zopezera chifuniro cha Mulungu zomwe ziri pa Aroma 12:1-2.

KUIKA TCHATI

Njira ina yolongosolera zinthu zomwe mwawerenga ndi kuziika mu tchati. Mupatsidwa matchati angapo kuti muwamalizitse ngati mbali imodzi ya phunziro ili. Matchati amathandiza kukumbukira mosavuta zomwe mwaphunzira.

Pali njira ziwiri zopangira tchati:

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera.

2. Kodi cholakwika ndi chani ndi mndandanda uli munsiu.

I. Mfundo yaikulu.

A. Iyi ndi mfundo yaing'ono yogwirizana ndi ndi mfundo yaikulu.

B. Iyi ndi mfundo yaikulu yachiwiri.

3. Kodi ndi njira zingati zimene mungagwiritse ntchito pofuna kujambula tchati?

4. Kodi kuika zizindikiro kumagwirizana bwanji ndi kusanthula Baibulo?

(Mayankho amafunso amenewa ali kumapeto kwa Buku limeneli)

POPITIRIZA KUPHUZIRA

1. Werengani Yakobo 3:2 ndipo malizitsani mndanda ulu pansiu:

LILIME LA MUNTHU

Ngati sitichimwa ndi lilime ndiye kuti: (werengani vesi 2)

A.

B.

2. Chitsanzo cha zinthu zazing'ono zamphamvu ndi:

A. Zogwirira mkhamwa ntchito yake ndi (Vesi 3)

i.

II.

B. Moto ochepa: (Vesi4)

I.

3. Lilime ndi laling'ono koma: (Vesi 5-6)

A. Limadzitamandira zinthu zazikulu

B. Ndi lodzala ndi uchimo wa dziko lapansi.

C.

D.

E.

2. malititsani tchatu ili munsimuyi imene ikufotokozera ndime ina ya Yakobo 3:2-6.

| LILIME | CHIFANIZO CHAKE |
|------------------|------------------------|
| Chitsanzo | zotsatira |
| Moto ochepa | |
| Lilime la munthu | |

CHAPUTALA 7

GAWO LACHITATU: KUSANTHULA BAIBULO MWALUSO

KUSANTHULA BAIBULO NDI BAIBULO

ZOLINGA:

Mukamaliza mutu uwu mukhala mukukwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kuzindikira zizindikiro za Mau a Mulungu zomwe zagwiritsidwa ntchito m’Baibulo
- Kusanthula Mau a Mulungu kugwiritsa ntchito Baibulo
- Kuzindikiro tsinde la Mau a Mulungu.
- Kusiyanitsa pakati pa mkaka ndi nyama ya Mau a Mulungu.

VESI LOTSOGOLERA

Munditsegulire maso, kuti ndipenye Zodabwiza za m'cilamulo canu.

(Masalimo 119:18)

CHIYAMBI

Njira yabwino yoyambira kusanthula Baibulo ndiko kudziwa zomwe Baibulo limanena zokhuza ilo lokha. Iyi ndiyo nkhani yaikulu mu chaputala chino. Mu chaputala chino muphunzira zizindikiro za Mau a Mulungu ndi zinthu zinthu zokhuza Mau a Mulungu zomwe zabvumbulutsidwa m’Baibulo.

M’maphunziro athu ambiri tikamatchula vesi timaleMBERATU vesilo mkati mwa phunzirolo kuti musataye nthawi kumakatsegula Baibulo. Izi sizinachitike mu phunziro lino pa zifukwa. Chimodzi mwa zolinga za chaputala chino ndiko kukupangani inu kuti muzolowere kugwiritsa ntchito Baibulo lanu, chotero tangoika mavesi opanda mau ake. Pamene mukuphunzira, gwiritsani ntchito Baibulo lanu kupeza ndi kuwerenga mavesi omwe aperekedwa.

Ngati kupeza mabuku a m’Baibulo kumakuvutani, onani mndandanda wa mabuku koyambilira kwa Baibulo lanu kuti muone tsamba lomwe buku lomwe mukufunalo likuyambira. Mukafikapo ndiye kuti muli mu chaputala 1, tsono fufuzani chaputala chomwe mukufuna ndi vesi lake:

Masalimo 119: 89

— — —

Buku

Chaputala

Vesi

TSINDE LA MAU A MULUNGU

Tsinde la Mau a Mulungu ndi Mulungu mwini. Werengani Masalimo 68:11. Izi zimatsindika kuti Mulungu ndiye mwini wa Mau a Mulungu. 1 Atesalonika 2:13 amafotokoza kuti Baibulo ndi Mau a Mulungu ndipo kuti tsinde lake si munthu ayi. Pamene Yesu amalankhula mu nthawi ya utumiki wake wa pansi pano, anatsindika kunena kuti tsinde la Mau ake ndi Mulungu. Onani Yohane 14:10 ndi 24; 17:8 ndi 14; ndi 3:34.

MBIRI YA MAU A MULUNGU

Baibulo limafotokozera bwino mbiri yake, kuyankha mafunso monga, “Kodi Mau akhala alipo kwa nthawi yaitali bwanji?” Werengani Ahebri 11:3. Lemba ili limatsindika kuti dziko lapansi linalengedwa ndi Mau a Mulungu. Werengani Genesisi 1 nkhani ya chilengedwe cha kumwamba ndi dziko lapansi ndipo muona kuti izi ndi zoonza. Mulungu anachita kulankhula kuti dziko likhalepo. Mutha kuwerenga zambiri za izi pa 2 Petro 3:5-7. Ahebri 1:3 amanena kuti Iye akhalabe akugwirizitsa dziko nanyamula zonse ndi mphamvu ya Mau ake. Masalimo 33:6 amanena kuti miyamba inapangidwa ndi mphamvu ya Mau a Mulungu.

Mulungu ndi wamuyaya. Alibe chiyambi alibe malekezere. Popeza kuti Mulungu ndi Mau ake sangasiyanitsidwe (Iye ndi Mau), ndiye kuti Mau akenso alibe chiyambi ngakhale malekezere. Monga Mulungu, Mau akenso akhala alipo kwamuyaya. Werengani Eksodo 20:1-17 m’Baibulo lanu. Iyi ndi nkhani yoyamba kuti Mulungu akugwiritsa ntchito munthu (Mose) kulemba Mau ake.

Werengani Yohane 1 m’Baibulo lanu. Onesetsani mavesi a 1-5 ndi 14. Ndime imeneyi ikumutichula Yesu kuti ndi Mau. Akuti Mauwa (Yesu) anali ndi Mulungu ndi anali Mulungu pachiyambi. Ikutitsimikizira momwe Mulungu ndi Mau ake analengera dziko.

Yesu wakhala alipo pamodzi ndi Atate, koma mu 14 akutiuzza momwe Mau (Yesu) anakhalira thupi nabwera kudzakhala pa dziko ngati munthu. Vesi 11-12 akukamba momwe anakanidwira ndi anthu ake omwe ndi momwe iwo akumulandira Iye angakhali ana ake.

MABUKU, MALIKASA, NDI MIYALA

Mau a Mulungu analengedwa mu njira zosiyana-siyana mzaka zonsezi. Analembedwa pa miyala ndi Mose (Eksodo 20:1-17) ndi pa miyala ikulu-ikulu pamene Israel analowa mu dziko la malonjezano (Deuteronomu 27:1-8).

Mau a Mulungu analembedwa m’bukhu (Deuteronomu 31:24-26) ndi pa malikasa (Yeremiya 36:2). Likasa ndi pepala lalitali lokhala ndi timitengo tokulungura mbali zonse ziwiri. Munthu akamalemba kapena kuwerenga likasa amayamba mbali imodzi nkumafunzulula mbali inayo uku akupita.

Mulungu anauzira ngakhale m’Mau ake. Onani Deuteronomu 31:19-22. Davide analemba Mau a Mulungu mwa ndakatulo ndipo amakhala akuimba nthawi zambiri. Bukhu la Masalimo ndi buku la matamando ndi nyimbo m’Baibulo.

KUUZIRIDWA KWA BAIBULO

Chinthu chimodzi chofunikira kwambiri chomwe Baibulo limaulura chokhuza Mau a Mulungu ndi chakuti Mau a Mulungu anauziridwa ndi Mulungu mwini. Kudzera m’kuuziridwa kwa Mzimu Woyera, Mulungu analankhula ndi amuna oyera kuti alembe uthenga wake.

Onani 2 Timoteyo 3:16-17 m’Baibulo lanu. Mavesi awa akutsimikizira kuti Mau a Mulungu ndi owuziridwa ndi Mulungu. Tikuonanso kuti ndi opindulitsa m’magawo anayi a moyo wa Chikhristu:

- a. Chiphunzitsa
- b. Chitsutsano
- c. Chikonzero
- d. Chilangizo m’chilungamo

Mavesiwa akuonetsera cholinga chachikulu cha Mau a Mulungu. Ndipo zotsatira zake nzakuti munthu wa Mulungu amakhala woyenera, wokonzeka kuchita ntchito iriyonse yabwino.

MAU A MUYAYA

Mabuku a dziko lapansi amakhala abwino kwa kanthawi kochepe. Mwachitsanzo, mabuku a zaumoyo amakhala aphindu kwa nthawi yochepe. Mankhwala kapena njira zatsopano zochizira

matenda zikapezeka, mabukuwo amakhala kuti atha ntchito. Pamene Mau a Mulungu ndi amuyaya komanso opindulitsa nthawi zonse. Anali ofunikira kalelo, ndi ofunikira lero, komanso adzakhala ofunikira mtsogolo (onani Masalimo 119:89).

Werengani 1 Petro 1:23. Vesi ili limaphunzitsa kuti sikuti Mulungu amakhala kwa muyaya kokha, komanso ndi a muyaya. Mulungu alipo ndipo adzakhhalapo. Timatumikira Mulungu wamoyo. Iye sangasiyanitsidwe ndi Mau ake. Popeza kuti Mulungu ndi wamoyo, Mau akenso ndi amoyo komanso opindulitsa ku nthawi zonse.

Werengani Yesaya 40:8. Vesi ili likutsimikizira kuti Mau a Mulungu adzakhala kwamuyaya. Sadzaonongeka ngati momwe zinthu za dziko lapansi zimaonongekera kuthupi.

MAGAWO AWIRI OFUNIKIRA

Baibulo limakamba za magawo awiri ofunikira kwambiri a Mau a Mulungu. Pali mkaka wa Mau a Mulungu ndi nyama ya Mau a Mulungu. Mkaka wa Mau a Mulungu ndi choonadi cha Mau chosavuta kumvetsa. Pamene nyama ya Mau ndi chiphunzitso chozama cha Mau a Mulungu chomwe chimabweretsa kukhwima muuzimu. Mutha kuwerenga zambiri za izi pa Ahebri 5:13-14 ndi 1 Petro 2:2.

ZOLINGA ZA MAU

Mulungu anapereka Mau ake kuti akakwaniritse zolinga zapaderadera. Ndipo zina mwa zolinga zimenezi ndi izi:

- Mau amalenga chikhulupiriro cha mu Uthenga Wabwino: Machitidwe 4:4
- Amayeretsa: Yohane 15:3; Aefeso 5:26.
- Ukamva Mau umakhulupirira nupeza moyo wosatha: Yohane 5:24
- Ndiye maziko a chiweruzo chosatha: Yohane 12:48
- Mizimu yoipa imasamutsidwa ndi Mau: Mateyu 8:16; Luka 4:36
- Zozizwitsa zimatsatira kulalikidwa kwa Mau kuchitira umboni choonadi cha Mau: Marko 16:20
- Amapereka chitsimikizo cha chipulumutso: 1 Yohane 1:2-6
- Munthu amabadwa mwatsopano mwa Mau: 1 Petro 1:23; Masalimo 119:41.

- Mau a Uthenga Wabwino ali m’Baibulo: 1 Yohane 5:7
- Munayeretsedwa ndi Mau: 1 Timoteyo 4:5
- Muli chiyembekezo m’Mau ake: Masalimo 130:5; 119:49, 81.
- Muli machiritso m’Mau ake: Masalimo 107:20
- Imakutetezani ku njira ya mdani woonongayo: Masalimo 17:4
- Mau ndi mzimu ndi moyo: Yohane 6:63
- Amabweretsa chimwemwe ndi kukondwera: Yeremiya 15:16
- Mau amaonjezera chikhulupiriro: Aroma 10:17
- Amabweretsa chitonhozo: 1 Atesalonika 4:18; Masalimo 119:50, 52
- Amakonzanso: 1 Timoteyo 4:6
- Amabweretsa mayankho a mapemphero: Yohane 15:7
- Ndi mfungulo ya chipambano: Yoswa 1:8
- Munthu amadalitsika akamamva ndi kuchita Mau: Luka 11:28
- Amapindulitsa m’kukula kwa moyo wauzimu: 2 Timoteyo 3:16-17
- Amabweretsa madalitso akasungidwa komanso matembelero akapanda kusungidwa: Deuteronomu 28
- Ndi chida champhamvu mnthawi ya mayesero: Mateyu 4
- Amapangitsa anthu wamba kukhala anzeru: Masalimo 19:7
- Amaunikira: Masalimo 19:8
- Amachenjeza: Masalimo 19:11
- Kusunga Mau kumabweretsa dalitso lalikuru: Masalimo 19:11
- Amatsegula makomo a kumwamba: Chibvumbulutso 22:14
- Amabweretsa mdalitso woyenda m’chiyero: Masalimo 119:11

- Amampanga munthu kukhala wamzeru kuposa adani ake, aphunzitsi, komanso makolo ake: Masalimo 119:98-104
- Amafulumizitsa: Masalimo 119:25
- Amalimbikitsa 119:28
- Ndi maziko a chifundo cha Mulungu pa munthu: Masalimo 119:58
- Amabweretsa kukondwa: Masalimo 119:92
- Amapereka nzeru kwa osazindikira: Masalimo 119:130
- Amabweretsa mamasulidwe: Masalimo 119:170

MAU A MULUNGU SI OPANDA PAKE

Monga taona kale, Mau a Mulungu ali ndi zolinga zambiri. Malemba amanena kuti Mau adzakwaniritsa cholinga chomwe anakhazikitsidwira. Werengani Yesaya 55:11. Apa Mulungu akutsindika kuti Mau ake sadzabwelera chabe kutanthauza kuti Mulungu salonjeza osakwaniritsa. Chomwe walankhula chimachitika. Liu liri lonse la Mau a Mulungu linalembedwa ndi cholinga ndipo cholingacho chidzakwaniritsidwa.

ZIZINDIKIRO ZA MAU

Baibulo limagwiritsa ntchito zizindikiro zosiyanasiyana pofotokozera Mau a Mulungu. Zizindikiro ndi zinthu zomwe zimaimilira chinthu china chake. Mwachitsanzo, mkango ndi chizindikiro cha ufumu. Zizindikiro zotsatirazi ndi zomwe zagwiritsidwa ntchito m’Baibulo pofotokozera Mau a Mulungu. Werengani mavesi omwe aperekedwawo:

Kalilore: Yakobo 1:23-27

Munthu akayang’ana pa kalilore amaona nkhope yake. Chimodzimodzinso Mau a Mulungu, monga kalilore, Baibulo limationetsera momwe moyo wathu wauzimu uliri.

Mbale ya madzi: Aefeso 5:26-27

Mbale ya madzi ndi mau omwe agwiritsidwa ntchito m’Baibulo pofotokozera chiyeretso chazimu chomwe timapeza kudzera m’Mau a Mulungu.

Nyali: Masalimo 119:105

Kuunika: Masalimo 119:105; 130; Miyambo 6:23

Nyali komanso kuunika zimathandiza munthu kuona pamene ali mu mdima. Mau a Mulungu amatipatsa chitsogozo chazimu ndi kutithandiza kupeza njira pamene tasokera mu uchimo.

Mvula: Yesaya 55:10-11

Madzi: Aefeso: 5:26

Mvula komanso madzi amabweretsa chitsitsimutso. Mau a Mulungu amayerkezedwa ndi mvula komanso madzi popeza amakutsitsimutsa moyo wanu wazimu.

Chakudya: Yeremiya 15:16; 1 Petro 2:1-2; 1 Akorinto 3:1-2; Ahebri 5:12-14.

Baibulo limayerkezedwa ndi chakudya chomwe chimathetsa njala yauzimu. Monga m'mene munthu amasowekera chakudya kuti azikula kuthupi, kuuzimu munthu amasowekera Mau a Mulungu kuti azikula. Magawo ena a Mau a Mulungu amatchedwa mkaka popeza ndi osavuta kuwamvetsa. Magawo ena amatchulidwa kuti nyama popeza ndi ovutirapo kuwamvetsa.

Mulungu akufuna inu musunthe kuchoka pa mkaka wa Mau kuti mufike pa nyama ya Mau ake. Izi zingakhale zosavuta ngati musanthula Mau ake pafupipafupi.

Moto: Yeremiya 23:29; 20-9

Moto umagwiritsidwa ntchito poyenga zitsulo. Umachotsa zosayenera zonse. Mau a Mulungu amagwiranso ntchito ngati moto m'moyo wanu wazimu kunyeketsa maganizo, mau komanso ntchito zonse zoipa.

Nyundo: Yeremiya 23:29

Nyundo imatha kuphwanya mwala zidutswazidutswa. Mau a Mulungu amatha kutenga mitima yoimitsidwa ndi uchimo, ndi kuiphwanya, komanso kuipanga kukhala yofewa m'dzanja la Mulungu.

Lumo lakuthwa konsekonse: Ahebri 4:12

Lumo ndi mpeni wakuthwa kwambiri umene madotolo amagwiritsa ntchito popanga munthu oparesoni kuchipatala. Mau a Mulungu amampanga munthu oparesoni yauzimu kumchiritsa matenda auzimu. Amachotsa zotupa ndi matenda ena onse m'moyo wazimu wa munthu.

Lupanga: Aefeso 6:17

Lupanga ndi chida choopsa kwambiri kuthupi. Mau a Mulungu omwe ndi lupanga lauzimu ndi chida chachikulu mu nkondo yolimbana ndi mdani, Satana.

Mankhwala: Masalimo 119:25

Monga m'mene mankhwala amachiritsira matenda a mthupi, Mau a Mulungu amagwira ntchito yochiritsa matenda auzimu.

Mbeu: Mateyu 13:1-23; Marko 4:1-20; Luka 8:4-15; 1 Petro 1:23; Yakobo 1:18

Mau a Mulungu ali monga mbeu. Akadzalidwa mu mtima wa munthu, ndipo akapeza chonde chabwino, amakula ndi kubala chipatso chabwino chاوزimu.

Uchi: Masalimo 19:10

Uchi ndi chinthu chotsekemera kwambiri pa dziko lapansi. Mau a Mulungu amayerekezedwa ndi uchi popeza ndi okoma kwambiri mwauzimu. Kusanthula Mau a Mulungu kumabweretsa kukoma kwauzimu m'moyo wanu.

Golide: Masalimo 19:9-10

Ku thupi, ndi mwala umodzi mwa miyala ya mtengo wapatali. Baibulo liri ngati golide popeza muli mau a mtengo wapatali kuuzimu.

KUFOTOKOZERA MAU

Kuphatikizapo zizindikiro zimenezi, Baibulo limapereka kufotokozera kwina kwa Mau a Mulungu. Mau a Mulungu ndi:

- Mzimu wa Moyo: Yohane 6:63
- Mau a moyo wosatha: Yohane 6:68
- Okoma: 1 Samuel 3:1
- Oyera: Miyambo 30:5; Masalimo 12:6; 19:7; 119:140
- Choonadi ndi ofatsa: Machitidwe 26:25
- Choodani: John 17:17; Akolose 1:5; Masalimo 119:142
- Owona kuchokera pachiyambi: Masalimo 119:160
- Oyesedwa: Masalimo 18:3

- Olungama: Masalimo 33:4; 19:8; 119:75
- Mau a moyo: 1 Yohane 1:1; Afilipo 2:6
- Mau a chipulumutso: Machitidwe 13:26
- Mau a chikhulupiriro: Aroma 10:8
- Angwiro: Masalimo 19:7
- Phungu: Masalimo 119:24
- Okhulupirika: Masalimo 119:86
- Okhazikika: Masalimo 119:89
- Cholowa: Masalimo 119:111
- Mau a chilungamo: Masalimo 119:123
- Olungama ndi okha ulupirika: Masalimo 119:138
- Owongoka: Masalimo 119:137
- Osangalatsa: Masalimo 119:143

MOMWE TINGAYANKHIRE KU MAU A MULUNGU

Kumva, kuwerenga kapena kusanthula Mau kokha sikokwanira. Baibulo limatiphunzitsa kuti tikuyenera kuchitapo kanthu tikamva Mau a Mulungu: Mukamva Mau mukuyenera ku:

- Kulola kuti agwere pa nthaka yabwino mu mtima mwanu: Marko 4, Luka 8, Mateyu 13
- Kumva ndi kuwachita kuti mukhale anzeru: Yohane 12:47
- Kuwasunga: Yohane 14:23
- Kukhulupirira Yesu kuti Mau a Mulungu akhale mwa inu: Yohane 5:38
- Kukhala m'Mau ake: Yohane 8:31
- Kukhala ndi moyo osati ndi mkate wokha komanso ndi Mau: Mateyu 4:4; Luka 4:4; Deuteronomo 8:3
- Kutama Mau ake: Masalimo 56:4, 10

- Kuthokoza chifukwa cha Mau: Masalimo 119:62
- Kukweza Mau ake ngakhale kuposa dzina lake: Masalimo 138:2
- Kulemba Mau ake pa mtima panu: Yakobo 1:21
- Kukhala wochita Mau osati wongomva kokha: Yakobo 1:22-23
- Kupempha chikhululukiro cha uchimo kuti Mau ake akhale mwa inu: 1 Yohane 1:10
- Kukhumba mkaka wa Mau ake: 1 Petro 2:2
- Kulola Mau a Mulungu kukhala mwa inu mokwanira: Akolose 3:16
- Kugawa Mau a Mulungu molunjika: 2 Timoteyo 2:5
- Kufufuza Malemba: Yohane 5:39; Machitidwe 17:11
- Kulengeza Mau ake: Masalimo 119:26-27
- Kusankha Mau ake: Masalimo 119:30
- Kukakamira Mau ake: Masalimo 119:31
- Kuthamanga njira ya Mau ake: Masalimo 119:32
- Kuwasunga: Masalimo 119:33
- Kuwatsatira: Masalimo 119:34
- Kukondwera mwa Mau: Masalimo 119:35; 70; 77; 143; 174
- Kuika mtima wanu ku Mau: Masalimo 119:36
- Kukhumba kuti akhazikitsidwe mu mtima mwanu: Masalimo 119:38
- Kuwakhumba: Masalimo 119:40
- Kuwagwiritsa ntchito poyankha ena: Masalimo 119:42
- Kuyembekezera mwa Mau: Masalimo 119:43, 47
- Kuwasunga kosatha: Masalimo 119:44
- Kufunafuna Mau ake: Masalimo 119:45

- Kukhala wokonzeka kuwalankhula pamaso pa atsogoleri: Masalimo 119:46
- Kulingalira pa Mau: Masalimo 119:48; 78; 148
- Osawakana: Masalimo 119:52
- Kuyenda molingana ndi chiphunzitso chake: Masalimo 119:59
- Osachedwa posunga Mau ake: Masalimo 119:60
- Osawaila: Masalimo 119:61, 83, 93, 153, 176
- Kusankha abwenzi omwe amaopa ndi kusunga Mau: Masalimo 119:63
- Kuwakhulupirira: Masalimo 119:66; 128
- Kuwasunga ndi mtima wanu wonse: Masalimo 119:69
- Kuwatenga kukhala a mtengo wapatali kuposa golide kapena siliva: Masalimo 119:72
- Kukhumba kuwaphunzira: Masalimo 119:73
- Kuyembekezera m'Mau: Masalimo 119:74; 81
- Kupeza chithonhozo mwa Mau: Masalimo 119:76; 82
- Kuwakhumba kuti absinthe mtima wanu: Masalimo 119:80
- Osawataya: Masalimo 119:87
- Kuwafunafuna: Masalimo 119:94
- Kuwalingalira: Masalimo 119:95
- Kukhumba kumva Mau a Mulungu: Masalimo 119:131
- Kuyenda molingana ndi Mau: Masalimo 119:133
- Kumva kuwawa mtima Mau a Mulungu akapanda kulemekezedwa: Masalimo 119:136; 158
- Kuchita mantha ndi Mau a Mulungu: Masalimo 119:161
- Kuwakonda: Masalimo 119:163, 165, 167
- Kulankhula Mau ake: Masalimo 119:172

UDINDO WATHU PA MAU

Kuphatikizapo pa momwe tingayankhire Mau a Mulungu, tilinso ndi udindo pa Mau. Mpingo woyamba unakwaniritsa udindo pamene umanka nulalikira Mauponseponse (Machitidwe 8:4; 13:49; 12:24). Anapempha Mulungu kuti awapatse kulimbika mtima (Machitidwe 4:29 ndi 31) ndipo Mau a Mulungu anafalikira pa dziko lonse lapansi chifukwa cha kudzipereka kwao (Machitidwe 6:7; 19:20).

Zomwe Baibulo likulankhula za udindo pa Mau a Mulungu ndi izi:

- Mukuyenera kulalikira Mau dziko lonse lapansi: Mateyu 16:15; Luka 24:47; Marko 16:15
- Ngati mwaphunzira Mau a Mulungu, muli ndi udindo wowaphunzitsa kwa anthu ena: Agalatiya 6:6
- Mukuyenera kulalikira Mau: 2 Timoteyo 4:2
- Mukuyenera kulankhula Mau mopanda mantha: Afilipo 1:4
- Mulungu amaika Mau ake mwa inu kuti mukawalankhule kwa anthu ena: Deuteronomo 18:18-19; Yesaya 51:16; Yeremiya 1:9; 3:12; 5:14; 26:12; Ezekiel 2:6-7.
- Musalankhule mau anu koma Mau a Mulungu: Yesaya 58:13
- Musamachita manyazi ndi Mau a Mulungu: Marko 8:38
- Mukuyenera kuphunzitsa Mau kwa ana anu: Deuteronomo 6:6-9

MACHENJEZO A M'MAU

Awa ndi ena mwa machenjezo omwe Mulungu akupereka okhuzana ndi Mau ake:

- Chizunzo chidzabwera Mau ake akalalikidwa: Marko 4:7
- Some people will even be killed because of their witness for the Word: Chibvumbulutso 6:9; 20:4.
- Mau a Mulungu atha kukhala opanda mphamvu mwa inu chifukwa cha miyambo ya anthu: Marko 7:13.
- Mutha kusokoneza Mau a Ambuye: Yeremiya 23:36.

- Mutha kuononga Mau a Mulungu: 2 Akorinto 2:17
- Mutha kugwiritsa ntchito Mau monyenga: 2 Akorinto 4:2

Baibulo limanena kuti tisakhulupirire mau onse omwe tikumva: Miyambo 14:15. Izi zikutanthauza kuti si alaliki onse omwe amalalikira Mau a Mulungu. Pali aphunzitsi onyenga ambiri omwe saphunzitsa konse Mau a Mulungu (Yuda 1). Mukuyenera kudzipatula nokha kwa anthu otere (1 Timoteyo 6:3-5). Aphunzitsi onyenga amaphunzitsa mau awo osati a Mulungu.

Amalankhulanso:

- Mau onama Yeremiya 29:23
- Mau opanda kanthu Aefeso 5:6
- Mau onyenga Akolose 2:4
- Mau opsyapsyalika 2 Petro 2:3
- Mau osinjirira 2 Petro 2:18; Juda 16
- Mau onyoza 3 Yohane 10

Pomaliza, Baibulo likutipatsa mau omaliza a chenjezo okuzana ndi Mau a Mulungu pa Chibvumbulutso 22:18-19.

(Chibvumbulutso 22:18-19)

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogoloera osonera

2. Lembani zizindikiro kapena zifanizo zisanu za Mau a Mulungu zomwe zagwiritsidwa ntchito m'Baibulo.

3. Pali zolinga zambiri za Mau a Mulungu zomwe mwaphunzira mu chaputala chino. Lembani zitatu zokha.

4. Chifukwa chiyani simukuyenera kukhulupirira mau ali onse omwe mukumva?

5. Kodi ndi chenjezo lotani lomwe laperekedwa kwa iwo amene amaonjezera Mau a Mulungu?

6. Nanga iwo amene amachotserako Mau a Mulungu apatsidwa chenjezo lotani?

7. Kodi tsinde la Mau a Mulungu ndi ndani? _____

8. Kodi Yesu amalankhula mau andani? _____

9. Magawo awiri a Mau a Mulungu ndi:

a. _____

b. _____

10. Molingana ndi mbiri ya Baibulo, kodi munthu woyamba kulemba Mau a Mulungu ndi ndani?

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto a bukhu lino).

KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

Mwa machaputala onse a m’Baibulo, Masalimo 119 amalankhula kwambiri za Mau a Mulungu. Komanso ndi chaputala chachitali kwambiri mwa machaputala onse a m’Baibulo.

Pali mau angapo omwe agwiritsidwa ntchito mu chaputala chino okhuza Mau a Mulungu. Nthawi zonse agwiritsidwa ntchito amaonjezera chidziwitso chathu cha Mau a Mulungu. Werengani Masalimo 119 ndi kudula mzere kungsi paliponse pomwe mupeze mau awa:

- Mau
- Malemba
- Ziweruzo
- Malamulo
- Chilamulo
- Njira yanu
- Mau a umboni wanu

Mukatero, werenganinso chaputalacho ndi kupanga tchatu chanu kuti mulembe Salimoli mwachidule. Tsatirani njira yaperekedwa m’musiyi. Lembani vesi iliyonse yomwe ili ndi mau amenewa ndipo mulembe ndemanga yanu kumapeto kwake pa mau amenewo.

Pitirizani njirayi:

VESI

NDEMANGA

Vesi 1

Ndife odala ngati tiyenda m’chilamulo chake

CHAPUTALA 8

KUSANTHULA MAU KOMANGILIRA MOYO WAUZIMU

ZOLINGA:

Pomaliza chaputala chino mukuyenera kukwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kulemba ndondomeko za kasantulidwe ka Mau komangilira moyo wauzimu.
- Kusanthula Mau komangilira moyo wauzimu

VESI LOTSOGOLERA

Maso anga anakumika malonda a usiku, Kuti ndilingirire mau anu.

(Masalimo 119:148)

MAU OYAMBA

Njira yoyamba posanthula Mau a Mulungu yomwe muphunzire ndiyotchedwa kusanthula Mau komangilira moyo wauzimu. Chaputala chino chitanthauzira, kufotokozera, komanso kupereka chitsanzo cha kasantulidwe ka Mau kongomangilira moyo wauzimu. Chigawo cha “Kupitiriza Kuphunzira” chikupatsani mwayi wakuti muchite zomwe mwaphunzira. Ndipo musanthula Mau mu njira imeneyi.

KUTANTHAUZIRA NJIRAYI

Njira yosanthula Mau a Mulungu momangilira moyo wauzimu inabwera kudzera m’ moyo wodzipereka kwatunthu pamaso pa Mulungu. Chotero njirayi imakuthandizirani inu kuti mukule nkudzipereka komanso kudziyereza pamaso pa Mulungu. Imakutsogolerani nkupembedza Mulungu mwakuya komanso kupanga ubale wanu ndi Yesu Khristu kukhala wabwino.

Kusanthula kwa mtundu uwu simumangothera pongosanthula komanso kugwiritsa ntchito zomwe mwapeza m’ moyo wanu wa tsiku ndi tsiku. Satana mdierekezi amadana kwambiri ndi njirayi ndipo amaonesetsa kuti isamachitike pa moyo wa Mkhristu. Iye salimbana nkungosanthula kuti munthu akhale ndi chidziwitso chabe koma kuti pamene munthu wayamba kugwiritsa ntchito zomwe waphunzirazo pa moyo wake wa tsiku ndi tsiku ndi kusinthika kwa

moyo wauzimu. Kumva Mau kokha sikokwanira. Tikuyenera kugwiritsa ntchito zinthu zomwe taphunzira kuchokera m’Mau a Mulungu osati kungophunzira basi osachitapo kanthu:

Khalani akucita mau, osati akumva okha, ndi kudziyenga nokha. Pakuti ngati munthu ali wakumva mau wosati wakucita, iyeyu afanana ndi munthu wakuyang'anira nkhope yace ya cibadwidwe cace m'kalirole; pakuti wadziyang'anira yekha nacoka, naiwala pompaja nali wotani. Koma iye wakupenyenera m'lamulo langwiwo, ndilo laufulu, natero cipenyere, ameneyo, posakhala wakumva wakuiwala, komatu wakucita nchito, adzakhala wodala m'kucita kwace. (Yakobo 1:22-25)

M’phunziro lino muphunzira njira zambiri za kasanthulidwe ka Mau a Mulungu. Koma mukuyenera kuchitapo kanthu pa njira iriyonse mungagwiritse ntchito posanthula Mau. Kaya musanthula bukhu, chaputala, vesi kapena liu, onesetsani kuti zomwe mwapezazo mukuzigwiritsa ntchito m’oyo kapena mu utumiki wanu.

KUFOTOKOZERA NJIRAYI

Gwiritsani ntchito fomu yomwe yaperekedwa m’chigawo cha “Kupiriza Kuphunzira” kuti musanthule nokha malemba momangilira moyo wanu wauzimu. Ndondomeko zotsatirazi zikuthandizani pa kusanthula kwanu:

SITEPE 1: LEMBANI ZINTHU ZOKHUZA NDIMEYO

Lembani dzina la bukhu lomwe mukupezeka ndime yomwe mukusanthulayo. Kenako lembani chaputala ndi vesi za ndime yomwe mwasankha kuti musanthule.

SITEPE 2: PEZANI MUTU WA NDIMEYO

Werengani ndime yomwe mwasankha kuti musanthuleyo. Pezani mutu womwe ukumangilira nkhani yonseyo ndi kulemba mutuwo mu tchatu chanu.

SITEPE 3: PEZANI VESI LOTSOGOLERA

Kodi ndi vesi iti yomwe ikuomba mkota kapena kuti kumangilira ndime yomwe mukusanthulayo? Lembani mau a muvesilo ndi vesi lake mu tchanu chanu.

SITEPE 4: OMBANI NKOTA (KULEMBA MWACHIDULE)

Mwa inu nokha, lembani mwachidule zomwe ndime ikuphunzitsa.

1. Lembani mndandanda wa mfundo zikuluzikulu zomwe mwapeza
2. Gwiritsani ntchito tchati polemba mwachidule ndimeyo
3. Lembani chiganizo chimodzi chachifupi chomangilira zomwe mwapezazo.
4. Lembani ndimeyo m' mau anu. Uku ndiko kulemba ndime monga momwe mwaimvera pogwiritsa ntchito mau anu osati omwe alembedwawo. Tsatirani ndimeyo polemba koma m'chilankhulo chanu. Onani gawo lachitsanzo.

SITEPE 5: LINGALIRANI

Kuwerenga ndi kusanthula Mau a Mulungu ndi chinthu cha mtengo wapatali koma mukuyenera muphunzirensa kulingalira Mau. Mau oti “kulingalira” amanthauza kuganizira, kukhazikikapo kapena kusinkhasinkha. Mukasankha ndime yoti musanthule, pezani mutu waukulu ndi vesi lotsogolera, lembani mwachidule zomwe mwaphunzira ndipo pomaliza lingalirani ndimeyo.

Mulungu anauza Yoswa kuti kulingalira pa Mau a Mulungu ndi njira ya chipambano:

Buku ili la cilamulo lisacoke pakamwa pako; koma ulingiriremo usana ndi usiku, kuti usamalire kucita monga mwa zonse zolembedwamo; popeza ukatero udzakometsa njira yako, nudzacita mwanzeru. (Yoswa 1:8)

Werengani modekha ndimeyo. Werengani mokweza. Tangoganizani kuti Mulungu akulankhula ndi inu kudzera mu uthenga umenewu. Onani zomwe ndimeyo ikunena molunjika moyo wanu pogwiritsa ntchito mafunso omwe ali pansu pa Sitepe 6 mu phunziro lino.

Njira ina yofunika kwambiri polingalira Mau ndi yoloweza pantima. Mukaloweza ndimeyo mudzatha kuikumbukira mosavuta mukayamba kuiganizira. Vesi lotsogolera munalemba lija ndi gawo labwino lakuti muloweze. Pangani timakhadi ting'onoting'ono monga momwe akunenera m'musimu. Lembani mau a vesilo mbali imodzi ya khadi, ndipo vesi yake mulembe kuseli kwake.

Mwachitsanzo:

Mbali imodzi lembani: *Ndinabisa mau anu mu mtima mwanu kuti ndisakuchimwireni*

Mbali inayo lembani: *Masalimo 119:11*

Werengani vesilo kangapo mokweza kunako yeserani kubwereza koma osaonera pa khadi. Mukatero onani pa khadi ngati simunalakwitse. Onaninso vesi lake kumbuyo kwa khadi kuti muone ngati mungakwanitse kutchula zonse nthawi imodzi. Sungani makhadi anu malo abwino kuti mupitirize kulingalira mavesiwo nthawi ina.

SITEPE 6: GWIRITSANI NTCHITO ZOMWE MWAPHUNIZRA PA MOYO WANU

Tsopano ndi nthawi yoti mugwiritse ntchito choonadi chomwe mwaphunzira pa moyo ndi utumiki wanu. Nthawi zina simungathe kugwiritsa ntchito zomwe mwaphunzira nthawi yomweyo, komabe yambani kutero m'mene mungathere. Mulungu akupatsani chisomo chakugwiritsa ntchito zomwe mwaphunzira ngakhale pang'ono pang'ono.

Mafunso otsatirawa akuthandizirani momwe mungagwiritsire ntchito Mau a Mulungu pa moyo wanu:

- **Chitsanzo choti mutsatire:**

Kodi pa ndimeyi pali chitsanzo chakuti nditsatire?

- **Cholakwika choti mupewe:**

Kodi pa vuto kapena tchimo lakuti mupewe?

- **Ntchito yoti muchite:**

Kodi ndimeyi ikundiiza kuti pali ntchito yoti ndichite? Nanga ndi ntchito yanji?

- **Lonjezo lakuti mulengeze:**

Kodi ndi lonjezo lanji lomwe ndingalengeze mu vesili?

- **Ubale woti umangidwe:**

Kodi ndimeyi ikukamba zotani za ubale wanu ndi Mulungu kudzera mwa Yesu Khristu?

Kodi ikuphunzitsa zotani zokhuza Mulungu Atate, Yesu Khristu, ndi Mzimu Woyera?

Kodi ndimeyi ikuphunzitsa zotani zokhuza ubale wanu ndi anthu ena m'banja, mudzi, mpingo wanu? Nanga za ubale wanu ndi inu eni, ikukuphunzitsa zotani?

- **Zofunika kusintha:**

Kodi pali chinthu chomwe mukuyenera kusintha molingana ndi ndime yomwe mwaphunzirayi? Pezani chinthu cheni cheni.

- **Pemphero loti mupemphere:**

Pempherani pemphero lanu lanu pa ndimeyi. Mufunzeni Mulungu akuthandizeni kuti mugwiritse zinthu zomwe mwaphunzira. Pempheroli likupangitsani kuona kuti zomwe mwaphunzirazi ndi zokhuza inu osati munthu wina. Muthanso kulemba pemphero lanu pamapeto pa zomwe mwalemba zija. Onani chitsanzo chomwe chaperekedwa mu chaputala chino.

CHITSANZO CHA KASANTHULIDWE KA MAU KOMANGILIRA MOYO WAUZIMU

SITEPE 1: LEMBANI ZINTHU ZOKHUZA NDIMEYO

Bukhu: Agalatiya

Chaputala: 5

Mavesi: 16-25

SITEPE 2: PEZANI MUTU WAUKULU MU NDIMEYO

Mutu: Ntchito za Thupi ndi Chipatso cha Mzimu

SITEPE 3: PEZANI VESI LOTSOGOLERA

Vesi Lotsogolera: Ngati tili ndi moyo ndi Mzimu, ndi Mzimunso tiyende. (Agalatiya 5:25)

SITEPE 4: OMBANI MKOTA (KULEMBA MWACHIDULE)

1. Chitsanzo cha mndandanda wamlozo wanu:

NTCHITO ZA THUPI NDI CHIPATSO CHA MZIMU

- I. Thupi lilakalaka potsutsana naye Mzimu, ndi Mzimu potsutsana nalo thupi. Iwo amene akhala monga mwa thupi sadzalowa mu Ufumu wa Mulungu. Ntchito za thupi ndi monga:
 - a. Chigololo
 - b. Chiwerewere
 - c. Chidetso
 - d. Kukhumba zonyasa

- e. Kupembedza mafano
- f. Nyanga
- g. Madano
- h. Magawano
- i. Ndeu
- j. Mkwiyo
- k. Kaduka
- l. Zotetana
- m. Mipatuko
- n. Njiru
- o. Kuledzera
- p. Mcezo
- q. Kuphana.

II. Chipatso cha Mzimu chomwe Mulungu akufuna kutipatsa chotsutsana ndi ntchito za thupi:

- a. Chikondi
- b. Chimwemwe
- c. Mtendere
- d. Kuleza mtima
- e. Chifundo
- f. Kukoma mtima
- g. Chikhulupiriro
- h. Chifatso
- i. Chiletso

- III. Tikuyenera kuti:
- a. Tiyende mwa Mzimu (vesi 16 ndi 25)
 - b. Titsogozedwe ndi Mzimu (vesi 18)
 - c. Tikhale mwa Mzimu (vesi 25)

2. Chitsanzo cha tchati yolembe ndime mwachidule:

NTCHITO ZA THUPI NDI CHIPATSO CHA MZIMU

| Ntchito za Thupi (Kufitsa zilakolako) | Chipatso cha Mzimu (Kukhala mwa Mzimu) |
|--|---|
| Chigololo | Chikondi |
| Chiwerewere | Chimwemwe |
| Chidetso | Mtendere |
| Kukhumba zonyasa | Kuleza mtima |
| Kupembedza mafano | Chifundo |
| Nyanga | Kukoma mtima |
| Madano | Chikhulupiriro |
| Magawano | Chifatso |
| Ndeu | Chiletso |
| Mkwiyo | |
| Kaduka | |
| Zotetana | |
| Mipatuko | |
| Njiru | |
| Kuledzera | |
| Mcezo | |

Kuphana

3. Chitsanzo cha mau owumba mkota kapena kuti kulemba mwachidule:

Ndimeyi ikutipatsa zinthu ziwiri zisiyana: Zilakolako za thupi ndi chipatso cha Mzimu. Ngati ndife a Yesu, tikuyenera kupachika zilakolako za thupi ndi kukhala, kuyenda, komanso kutsogozedwa ndi Mzimu Woyera.

4. Chitsanzo cha kulemba mwa inu nokha Agalatiya 5:24-25.

“Iwo okhala mwa Khristu aononga zokhumba, zokonda komanso zilakolako za thupi. Ngati tinena kuti Mzimu Woyera ali mwa ife, tikuyenera kuchita zinthu motero”

SITEPE 5: KULINGALIRA NDIME

Mavesi oti muloweze: vesi 16-18 ndi 25-26. Lowezaninso mndandanda wa chipatso cha Mzimu chimene Mulungu akufuna kuti chikhazikike m’ moyo wanu. Lingalirani ndi kusanthula tanthauzo la chipatso chiri chonse cha Mzimu Woyera. Mwachitsanzo, kodi kukhala wofatsa, wokoma mtima, woleza, kapena wodziletsa kumatanthauza chiani?

SITEPE 6: KUGWIRITSA NTCHITO ZOMWE MWAPHUNZIRA

Chitsanzo choti mutsatire: Kukuza chipatso cha Mzimu Woyera m’ moyo wanga.

Cholakwika choti ndipewe: Ntchito za thupi

Ntchito yoti ndichite:

- a. Kuyenda mwa Mzimu vesi 16 ndi 25
- b. Kutsogozedwa ndi Mzimu vesi 18
- c. Kukhala mwa Mzimu vesi 25

Lonjezo loti mulengeze: “Komai chi ndinena kuti, muyendeyende mwa Mzimu kuti musafitse zilakolako za thupi” (vesi 16).

Maubale ofunika kumangilira: Madera atatu ofunika kwambiri kusintha. Ubale wanga ndi anthu ena ukuyenera kuonetsera chikondi, kupirira, kufatsa ndi kuleza. Ndikuyenera ndikhalenso ndi chimwemwe, mtendere, kukoma mtima, chikhulupiriro ndi kudziletsa m’ madera onse a moyo wanga. Ndaphunzira kuti Mulungu amafuna kuti chiyero chikhale maziko a ubale wanga ndi

Iye. Ngati ndinedi wa Khristu, ubale wanga ndi anthu ena, Mulungu komanso ine mwini ukhala wosinthika.

Zofunika kusintha: Magawo atatu ofunika kwambiri kusintha:

- a. Kudziletsa: madyedwe, zokhumba za thupi, komanso m'makhalidwe.
- b. Chikhulupiriro: Ndizikhulupirira malonjezano a Mulungu.
- c. Chikondi: Wonetsani chikondi kwa iwo owoneka osakondeka.

Pemphero loti mupemphere:

Mulungu atate wa kumwamba. Ndithandizeni kuti ndiyende mwa Mzimu, ndi kukhala nthawi zonse mu Mzimu wanu. Yeretsani moyo wanga ku ntchito zonse zathupi. Ndithandizeni kuti ndipachike ntchito zonse zathupi. Ndipo mukuze chipatso chokoma cha Mzimu Woyera mwa ine.

Mu dzina la Yesu, Amen.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera osonera

2. Kodi kusanthula Mau komangilira moyo wauzimu ndi chiyani?

3. Lembani masitepe 6 a kasanthulidwe ka Mau komangilira moyo wauzimu?

4. Kodi kukhala “wochita mau” osati “ongomva” kumatanthauza chiyani? Perekani vesi yophera mphongo yankho lanu.

5. Ndi chifukwa chiyani Satana amalimbana kwambiri ndi njira imeneyi ya kasanthulidwe ka Mau?

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto kwa bukhu lino)

KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

Santhulani Afilipi 4:4-9 pogwiritsa ntchito njira ya kusanthula Mau yomangilira moyo wauzimu. Gwiritsani ntchito ndondomeko ili m'musiyi posanthula ndimeyi ndi ndime zina zonse mungasanthule ndi njira imeneyi.

KUSANTHULA BAIBULO MU NJIRA YOMANGILIRA MOYO WAUZIMU

Bukhu: Chaputala: Mavesi: Mutu waukulu:

Vesi Lotsogolera:

Mkota:

Kulingalira:

Kagwiritsidwe ntchito:

Chitsanzo chotsatira:

Zofunika kupewa:

Ntchito yofunika kuchita:

Lonjezo lofunika kulengeza:

Ubale wofunika kumanga:

Zofunika kusintha:

Pemphero loti ndipemphere:

CHAPUTALA 9

KUSANTHULA BUKHU

ZOLINGA

Pomaliza chaputala mutha kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kufotokozero momwe mungasanthulire bukhu la m’Baibulo
- Kusanthula bukhu la m’Baibulo
- Kulemba tchati cha kusanthula bukhu
- Kulemba mlozo wa bukhu la m’Baibulo

VESI LOTSOGOLERA

Mnyamata adzayeretsa mayendedwe ace bwanji? Akawasamalira monga mwa mau anu. (Masalimo 119:9)

MAU OTSOGOLERA

Mu chaputala chino muphunzira momwe mungachitire kafukufuku wa bukhu la m’Baibulo. Muphunziranso kulemba tchati cha bukhu la m’Baibulo ndi mlozo womwe ungaonetse zomwe mwasanthula mwachidule. Chitsanzo cha kasanthulidwe ka buku la m’Baibulo chaperekedwa mu gawo la “Kupiriza Kuphunzira” ndipo mukhala ndi mwayi woti mupange nokha. M’machaputala otsatirawa muphunzira kasanthulidwe ka machaputala, ndime, mavesi ndi mau a bukhu lomwe mukusanthula.

Kafukufuku wa bukhu ndi chitsanzo cha kusanthula mau Baibulo mwapamwambamwamba. Kutanthauza kuti timangodutsamo ndi cholinga choti tikhale ndi chithunzithunzi cha zomwe ziri m’bukulo. Kenako tiligawa bukhu lija ndi kuyamba kulisanthula machaputala, ndime, mavesi ndi mau ake. Pamenepo timakhala kuti tayambano kusanthula Baibulo “mozama.” Uku ndiko kusanthula chinthu pachokha pachokha kuti tione momwe chiliri. Ndipo kasanthulidwe aka ndi kosiwana ndi koyamba kaja kongodutsamo pamwambamwamba.

TANTHAUZO LA NJIRAYI

Kusanthula bukhu palokha ndi kofunika chifukwa machaputala, ndime, mavesi ndi mau ake amayenera kutanthauziridwa molingana nkhani zomwe zikukambidwazo. Ndipo kusanthula bukhu lonse kumathandiza kuti mudziwe nkhani zomwe zikukambidwa m’bukhu lonse kuti kutanthauzira kwanu kukhale koyenera.

KUFOTOKOZERA NJIRAYI

Pali masitepe atatu a kasanthulidwe ka bukhu la m’Baibulo:

SITEPE 1: KAFUKUFUKU WOYAMBILIRA

Werengani bukhu lonse nthawi imodzi kuti mupeze mutu kapena nkhani yaikulu m’bukhulo. Sankhani mutu womwe ungamangalire nkhani yonseyo. Mutu umene musankhewu ndi umene ukhale pamwamba pa tchati kapena mlozo wanu.

Yesani kupeza cholinga chenicheni cha bukhulo, anthu omwe adalembedwera, komanso amene analemba. Mabuku ena amanena yemwe analemba pamene ena timachita kukawerenga mabuku ena kuti tipeze yemwe analemba bukhu lomwe tikusanthulalo. Wolemba wina aliyense amakhala kuti ali ndi cholinga cholemba bukhulo motsogozedwa ndi Mzimu Woyera. Ndipo cholinga chimenechi chimaonetseredwa mkatikati mwa zolembedwa m’bukhulo.

Pezaninso malo kapena dera lomwe kunali munthu wolembayo pamodzi ndi omwe anawalembawo. Kutero kumathandiza kukhala ndi chithunzithunzi cha komwe kapena momwe zinthu zimene tikuwerengazo zidachitikira. Ndipo lembani deralo pamwamba pa tchati chanu.

Lembani mwachidule mfundo yaikulu ya moyo kapena utumiki yomwe yaonetseredwa (chiganizo chimodzi). Iyi ndi mfundo yaikulu yomwe mutenge kuchokera nkusanthula kwanu kwa bukhulo ndi kuigwiritsa ntchito pa moyo ndi utumiki wanu. Bukhu limodzi litha kukhala ndi mfundo zambirimбири, koma yesetsani kuti mupeze yomwe iri yofunikira kwambiri pa zonsezo.

Kumbukirani kuti machaputala a m’Baibulo sanauziridwe, anaikidwa ndi anthu wamba kuti atithandi nkawerengedwe ndi kasanthulidwe ka Baibulo. Mukawerenga bukhu lonse mosayang’ana machaputala, ndiye kuti mwaona uthenga wonse wam’bukhulo momwe udaperekedwera pachiyambi pomwe.

Musakhale ndi chidwi ndi zinthu zambiri mu sitepe yoyambayi. Fufuzani bukhuli kuti mungodziwa: Mutu waukulu, amene adalemba, cholinga, olemberedwa, komwe anthuwo amakhala, ndi mfundo yaikulu ya m'moyo ndi utumiki. Ndipo muwerenge mongofuna kudziwa zimenezi. Musaima ndikuyamba kulingalira zomwe mwawerengezo popeza nthawi yake si imeneyo. Izo muchitabe kutsogoloku.

SITEPE 2: TCHATI YA KASANTHULIDWE KA BUKHU

Werenganinso bukhulo kachiwiri. Onani magawo akuluakulu omwe ali m'bukhulo. Magawo amenewa atha kukhala ndi nkhani, mitu, malo, komanso zochitikika zomwe zapangitsa kuti akhalepo.

Pangani mitu ya chaputala chirichonse cha bukhu. Mutuwo ukhale kuti ukuchokera mu zomwe ziri m'chaputala chimenecho komanso wolunjika kuti usafanane ndi wamachaputala enawo. Mitu imeneyi ndiwo maziko a zomwe chaputalacho chikulankhula. Ikhale yaifupi kuti muzitha kukumbukira mosavuta. Lembani mitu ya machaputalayi mu tchati chanu cha kasanthulidwe ka bukhu.

Sankhani vesi lotsogolera la bukhu lonse. Vesili likhale kuti ndi tsinde la cholinga ndi zonse zomwe zalembedwa m'bukhumo. Ndipo lembani vesilo mu tchati chanu.

Pamene mukuwerenga, onani anthu omwe akukambidwa kwambiri m'ndimezo ndi kulemba maina awo m'tchati chanu. Mndandanda wa mainawu utithandiza pamene tiyambe kusanthula anthu a m'Baibulo. Muphunzira kasanthulidwe kake kutsogolo kwa phunziro lino.

Lembani mau ndi ziganizo zotsogolera mu tchati chanu. Izi zikuthandizani mu kamvetsedwe kanu ka bukhulo. Nthawi zambiri mau kapena ziganizozzi zimakhala kuti zabwerezedwa kapena kufotokozeredwa mwatsatanetsatane m'bukhulo. Mutha kugwiritsa ntchito mau amenewa pa kasanthulidwe ka mau komwe muphunzire posachepa.

SITEPE 3: MLOZO WA BUKHU

Gawo lomaliza nkasanthulidwe ka bukhu ndi kupanga mlozo wa bukhulo. Werenganinso bukhulo. Pamene mukuwerenga pangani mlozo wa bukhu lonse. Magawo ndi machaputala ena omwe mwalemba mu tchati chanu atha kukhala othandiza popeza mfundo zikuluzikulu za mlozo wanu. Cholinga cha mlozowu ndi kulemba mwachidule zonse zomwe ziri m'bukhulo.

CHITSANZO CHA NJIRAYI

SITEPE: KAFUKUFUKU WOYAMBILIRA

Bukhu: Bukhu lomwe tasankha kuti tisanthule ndi Afilipo.

Mutu: Pempho lakuti tikhale a mtima umodzi mwa Khristu.

Wolemba: Analemba ndi Mtumwi Paulo

Wolemberedwa: Analemba Akhristu a mpingo wa ku Afilipi.

Cholinga: Cholinga chake chiri magawo awiri. Analemba kuti athokoze Afilipo pa ntchito yawo yothandiza utumiki komanso kulimbikitsa umodzi.

Mau akuluakulu: Kondwerani, chimwemwe.

Vesi Lotsogolera: Afilipi 2:2

Anthu omwe akutengapo mbali: Uyod

Mfundo ya moyo ndi utumiki: Mfundo yaikulu ya moyo ndiyakuti umodzi wa mwa Khristu umabweretsa chimwemwe.

SITEPE 3: MLOZO WA BUKHU

Afilipi: Kulimbikitsa umodzi mwa Khristu

Mau Otsogolera:

- A. Malonje 1:1-2
 - 1. Kuchokera kwa Paulo ndi Timoteyo.
 - 2. Kupita kwa: Okhulupirira mwa Khristu Yesu, oyang'anira ndi atumiki ku Afilipi.
- B. Pemphero lopita kwa Afilipo 1:3-11
- C. Nkhani zapadera 1:12-26
 - 1. Zinthu zomwe zathandizira kuti Uthenga upite chitsogolo 1:12-18

2. Chikhulupiriro chakuti adzamasulidwa – 1:19-21
 3. Kufunsa kwake kuti chabwino ndi chani kufa kapena kumwalira 1:22-26
- II. Kulimbikitsa umodzi 1:27-2:18
 - A. Kupempha umodzi nthawi ya masautso 1:27-30
 - B. Umodzi mwa Khristu 2:1-11
 - C. Kukula muuzimu kumabweretsa umodzi 2:12-18
 - III. Zilinganizo za Paulo 2:19-30
 - A. Chiyembekezo chakutumiza Timoteyo 2:19-23
 - B. Chiyembekezo chakuti abwere yekha 2:24
 - C. Kutumiza Epaprodito 2:25-30
 - IV. Machenjezo 3:1-4:1
 - A. Motsutsana ndi aphunzitsi a Chiyuda 3:1-16
 - B. Motsutsana ndi aphunzitsi onyenga 3:17-21
 - V. Zilimbikitso 4:1-9
 - A. Umodzi pakati pa Uodiya ndi Suntuke 4:1-3
 - B. Umodzi m'chimwemwe 4:4
 - C. Umodzi m'kufatsa 4:5
 - D. Umodzi m'pemphero 4:6
 - E. Umodzi m'malingaliro 4:7-8
 - F. Umodzi pakati pa chidziwitso ndi ntchito 4:9
 - VI. Kuthokoza chifukwa cha mphatso yawo 4:10-20
 - VII. Mau omaliza 4:21-23
 - VIII. Anthu opezeka mu nkhani: Eudiya, Sunteke, Klement Epafrodito, ndi nyumba ya Caesara.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera osonera

2. Lembani nambala ya matanthauzo omwe aperekedwawo (1 ndi 2) pa mtundu wa kasanthulidwe koyenera.

Mtundu wa Kusanthula

Tanthauzo

_____ Mozama

1. Kusanthula mwapamwambamwamba

_____ Mongodutsa

2. Kusanthula mwa tsatane tsatane.

3. Lembani masitepe atatu a njira yasanthulira bukhu la m'Baibulo.

4. Kodi zinthu zisanu ndi chimodzi zofunikira kwambiri pochita kafukufuku woyambilira wa bukhu ndi ziti?

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto kwa bukhu lino).

KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

Sankhani bukhu limodzi kuchokera mu Chipangano Chatsopano kuti mulisanthule. Popeza kuti nkuyamba, sankhani bukhu lomwe ndi lalifupi. Gwiritsani ntchito ndondomeko za kasanthulidwe ka bukhu zomwe mwaphunzira mu chaputala chino. Lembani mwachidule ndemanga zanu pogwiritsa ntchito tchati ndi mlozo. Onani momwe tachitira m'musimu kuti muchite chimodzimodzi popanga tchati ndi mlozo wanu.

TCHATI CHA KUSANTHULA BUKHU

Dzina la bukhu:

Mutu wa Tchati

Machaputala

| 1 | 2 | 3 | 4 | 5 | 6 | 7 | 8 | 9 | 10 | 11 | 12 | 13 | 14 | 15 | 16 | 17 | 18 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|----|----|----|----|----|----|----|----|----|
| | | | | | | | | | | | | | | | | | |

Chapter Titles

Wolembe:

Olembredwa:

Cholinga:

Mau akuluakulu:

Vesi Lalikulu:

Anthu opezekamo:

Mfundo yaikulu m'moyo ndi mu utumuki:

CHAPUTALA 10

KUSANTHULA CHAPUTALA

ZOLINGA:

Mukamaliza chaputala chino mukuyenera kukwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera.
- Kulemba njira zinayi za kusanthulidwe ka chaputala
- Kusanthula Baibulo mu njira ya machaputala
- Kulemba tchatu cha chaputala kuti musonkhanitse maganizo anu mwachidule.
- Lembani mlozo wa chaputala

VESI LOTSOGOLERA

**Ndinabisa mau anu mu mtima mwanu kuti ndisakuchimwireni inu
(Masalimo 119:11).**

MAU OYAMBILIRA

Mu chaputala chapitachi mwaphunzira za momwe mungasanthulire bukhu la m’Baibulo.

Tsopano muphunzira kusanthula chaputala cha m’Baibulo. Chitsanzo cha kusanthula chaputala chaperekedwa mu chigawo cha “Kupitiriza Kuphunzira” kumapeto a chaputala chino.

KUTANTHAUZIRA NJIRA

Kusanthula chaputala ndi njira yosanthula Baibulo chaputala ndi chaputala.

KUFOTOKOZERA NJIRA

SITEPE 1: SANKHANI CHAPUTALA CHOTI MUSANTHULE

Lembani pa tchatu panu dzina la bukhu ndi chaputala chomwe mukusanthula. Werengani chaputala chonse ndipo pezani mutu waukulu mu chaputala chimenecho. Ngati mwachita kale kusanthula kwa bukhu la m’Baibulo ndiye kuti muli kale ndi mutu waukulu wa chaputala chimenechi.

SITEPE 2: IKANI ZIZINDIKIRO PA MAGAWO A NDIME

Ikani zizindikiro mu ndime zomwe ziri m’machaputala. Ma Baibulo ena amaikiratu magawo a ndime amenewa. Izi ndi zomwe zimaonetsera pomwe payambira nkhani ndi pomwe ikuthera. Kenako nkupita ku gawo la ndime lina. Ngati Baibulo lanu lilibe, mutha kudziikira nokha pongozungulizira nambala ya vesi yomwe iri koyambilira kwa ndime iriyonse.

SITEPE 3: PANGANI TCHATI CHA CHAPUTALA

Pa tchati cha chaputala lembani mutu wa chaputalacho. Lembani mavesi omwe akupanga magawo a ndime mu chaputala chimenecho. (Onani chitsanzo). Ndime iriyonse ipatseni mutu womwe ukuonetsera zomwe ziri mu gawo la ndime imeneyo. Gwiritsani ntchito mbali yomwe mukulemba ndemanga zanu kuti mulembepo zomwe mukuganiza pa gawo limenelo (onani chitsanzo). Ndemanga zimenezi zikuthandizani pamene muzilemba mlozo wa chaputala.

SITEPE 4: LEMBANI MLOZO WA CHAPUTALA

Mu chaputala chapitachi mwaphunzira za kulemba mlozo wa bukhu lonse la m’Baibulo. Tsopano mupanga mlozo wa chaputala. Mwasankha kale mutu wa chaputala pamene mumapanga tchati cha chaputala chanu. Gwiritsani ntchito mutu umenewo popanga mlozo. Gwiritsani ntchito magawo a ndime ndi mitu ya ndime popanga mfundo zikuluzikulu. Kenako sankhani mfundo zing’ono zing’ono ndi kuika mlozo komanso mavesi mu ndime iriyonse ya chaputalacho. Ikani mavesiwo molingana ndi mfundo zikuluzikulu ndi mfundo zing’onozing’ono. Muthanso kuika mavesi ena a m’Baibulo omwe akugwirizana ndi mutuwo ndipo muwafotokozere bwino (onani chitsanzo). Machaputala ena ndi ataliatali chotero, ngati malo achepa pitirizani pa pepala lina.

CHITSANZO CHA NJIRA

Tasankha bukhu la Yuda, lomwe liri ndi chaputala chimodzi chokha, kuti tigwiritse ntchito ngati chitsanzo pa phunziro lathu la kusanthula chaputala.

SITEPE 1: SANKHANI MUTU WA CHAPUTALA

Mutu womwe tasankha mu chaputala cha m’Yuda ndi wakuti, “Chenjezo pa Aphunzitsi Onyenga.”

SITEPE 2: IKANI ZIZINDIKIRO ZA MAGAWO A MACHAPUTALA

Chaputalachi chagwawidwa m'magawo a ndime zingapo kuyambira vesi 1, 3, 4, 5, 8, 11, 12, 14, 16, 17, 19, 20, 22, 24. Mavesi amenewa anazungulizidwa poika zizindikiro mu ndime zomwe ziri mu chaputalachi.

SITEPE 3: LEMBANI TCHATI CHA KUSANTHULA CHAPUTALA

Chitsanzo cha tchati cha kusanthula chaputala ndi ichi:

Tchati cha Kusanthula Chaputala

Book: Yuda Chaputala: 1 Mutu wa Chaputala: Chenjezo pa Aphunzitsi Onyenga

| Mavesi | Mutu wa Ndime | Ndemanga |
|---------------|----------------------------|----------------------------------|
| 1-2 | Malonje | Wolemba ndi Yuda |
| 3 | Cholinga | Kumenyera nkhondo chikhulupiriro |
| 4 | Amuna ena | Kupeza makhalidwe asanu a anthu |
| 5-7 | Mbiri | Israel, Angel, Sodom ndi Gomora |
| 8-10 | Kufotokozero kunayamba | Makhalidwe asanu ena a anthu |
| 11 | Kufotokozero mwa chitsanzo | Kaini, Abele ndi Kore |
| 12-13 | Kufotokozero moyerekeza | Mawanga mu maphwando ndi zina |
| 14-15 | Chiweruziro cha mtsogolo | Cha Ambuye ndi oyera mtima |
| 16 | Kufotokozero kupitilira | Makhalidwe asanu ena |
| 17-18 | Kumbukirani Mau | Chenjezo la Yesu |
| 19 | Kufotokozero kupitilira | Makhalidwe ena atatu |
| 20-21 | Kupewa chinyengo | Dongosolo la mfundo zinayi |
| 22-23 | Momwe tingathanirane nawo | Magawo awiri |
| 24-25 | Mau omaliza | Tikhoza kusungika ku zoipazi |

SITEPE 4: PANGANI MLOZO WA CHAPUTALA

Uwu ndi mlozo chaputala womwe tinapanga kuchokera nkusanthula kwathu kwa Yuda:

Mlozo wa Chaputala cha Yuda: Chenjezo pa Aphunzitsi Onyenga

- I. Mau Oyamba: Malonje 1:1-2
 - A. Kuchokera: Jude
 - 1. M'bale wa Yakobo.
 - 2. Kapolo wa Yesu.
 - B. Kupita kwa:
 - 1. Oyeretsedwa ndi Mulungu.
 - 2. Osungika mwa Khristu.
 - 3. Oyitanidwa.
- II. Cholinga: 1:3
 - A. Cholinga choyambilira: Chipulumutso cha wamba.
 - B. Cholinga china: Kupempha kuti amenyere nkondo chikhulupiriro.
- III. Makhalidwe a “amuna ena” (aphunzitsi onyenga): 1:4
 - A. Anakwawira mozemba.
 - B. Anaikidwiratu kuti akaweruzidwe.
 - C. Amuna opanda uMulungu.
 - D. Osandutsa chisomo cha Mulungu kukhala chilakolako chonyansa.
 - E. Okana Ambuye Yesu Khristu.
- IV. Nkhani zitatu zochokera mu mbiri yakale: 1:5-7
 - A. Israel: Yemwe anapulumutsidwa, kenako nkuonongedwa: 5 (Numeri 13-14 ndi 1 Akorinto 10:5-10)
 - B. Angelo: Anasiya malo awo kumwamba, anasungidwa m'maunyolo: 6 (2 Petro 2:4)
 - C. Sodomu ndi Gomora: Tchimo linabweretsa chilango cha moto: 7 (Genesisi 18-19)
- V. Kufotokozera aphunzitsi onyenga 1:8-10 (kupiriza kufotokozera kuchokera mu vesi 4)

- A. Olota maloto: 8
 - B. Odetsa thupi: 8
 - C. Opeputsa maufumu: 8
 - D. Ochitira mwano maulemelo: 8-9
 - 1. Mikael sanalankhule mwano ngakhale kwa Mdierekezi.
 - 2. Amuna awa amachitira mwano ngakhale zinthu zimene sazidziwa.
 - E. Apotoza dala chilengedwe: 10
- VI. Kufotokozerera amuna abodza mwa chitsanzo: 1:11
- A. Njira ya Kaini: Anakana mwanzi ngati njira yoyenera ku kukhululukidwa kwa machimo (Genesisi 4).
 - B. Kulakwitsa kwa Balamu: Kuchita utumiki kuti upeze chuma. (Numeri 22-24)
 - C. Kulankhula kwa Kore: Kukana utsogoleri woyikidwa ndi Mulungu (Numeri 16)
- VII. Kufotokozerera amuna oipawa mwa mkuluwiko (kuwayerekeza ndi zitsanzo za chilengedwe) 1:12-13
- A. Mawanga kapena miyala m'maphwando anu (mu chakudya).
 - B. Mitambo: Kulonjeza zambiri koma osachita kanthu; kumangotengeka ndi mphepo kupita uku ndi uku.
 - C. Mitengo: Yopanda chipatso, kapena mitsitsi kuti ikhazikike; kufa pawiri: Kufa mu uchimo komanso kufa m'chinyengo.
 - D. Mafunde: Amphamvu, aphokoso koma opanda phindu.
 - E. Nyenyezi: Zooneka zowala, koma zosungidwa mu mdima.
- VIII. Chilango cha mtsogolo choneneredwa ndi Enoki: 1:14-15 (Genesisi 5:18-24)
- A. Oweruzidwa ndi Ambuye pamodzi ndi oyera mtima zikwi khumi
 - B. Chifukwa cha ntchito zawo zonse zoipa zimene anachita.

- C. Chifukwa cha zamwano zonse analankhula pamaso pa Mulungu.
- IX. Kufotokozeredwa kwa anthu oipa kukupitilira: 1:16-17
- A. Ong'ung'uza.
 - B. Odandaula.
 - C. Oyenda mwa zilakolako zawo zoipa.
 - D. Pakamwa polankhula mau oipa ndi odzitamandira.
 - E. Otamanda anthu nayesa anthu ena kukhala oposa amnzawo chifukwa cha chuma, mphamvu ndi maudindo.
- X. Kumbukirani: Yesu anachenjeza: 18-19
- A. Anthu onyoza adzadza m'masiku omaliza.
 - B. Nayenda monga mwa zilakolako zosapembedza.
 - C. Adzazipatula okha (m'magulu ndi mitundu).
 - D. Adzakhala ndi maganizo achikunja.
 - E. Sadzakhala ndi Mzimu wa Mulungu.
- XI. Dongosolo la mfundo zinayi zopewera kusokeretsedwa ndi anthu: 1:20-21
- A. Dzimangilireni nokha m'chikhulupiriro: 20
 - B. Pemphererani Mzimu Woyera: 20
 - C. Dzisungeni nokha mchikondi cha Mulungu: 21
 - D. Yang'anirani chisomo cha Ambuye Yesu Khristu: 21
- XII. Momwe tikachitire ndi anthu oipa: 1:22-23:
- A. Pa ena muwachitire chifundo: 22
 - 1. Musiyanitse pakati pa omwe ndi ofooka chabe ndi iwo amene asankha kukhala oipa.
 - B. Koma ena muwapulumutse ndi mantha: 23
 - 1. Akwatuleni mu uchimo kapena moto.

2. Mudane ndi chovala chodetsedwa:

XIII. Mau omaliza: 1:24-25

- A. Ali nako kuthekera kotisunga ife kuti tisalephere: 24
 1. Kutipereka ife opanda chilema.
 2. Pamaso pa ulemelero wake.
 3. Ndi chimwemwe chachikulu.
- B. Kwa Mulungu m' modzi wa nzeru ndi Mpulumutsi wathu, mpaka muyaya: 25
 1. Ulemelero.
 2. Ukulu.
 3. Mphamvu.
 4. Ulamuliro.

KUGWIRITSA NTCHITO MAFUNSO

Kuphunzira kufunsa mafunso kutha kukuthandizani kuti musanthule bwino ndime za m' Baibulo. Mndandanda wa mafunso uli m' musiwu ndi wa mafunso a chaputala cha Yuda chomwe tikusanthula ndipo aperekedwa ngati chitsanzo. Umu ndi momwe mungaphunzilire kufunsa mafunso okuthandizani pa kusanthula Mau a Mulungu.

Vesi 1-2:

Kodi analemba kalatayu ndi ndani?

Ndi ubale wanji ndi Yesu womwe waperekedwa?

Ndi ubale wanji ndi Yakobo womwe waperekedwa?

Ndi njira zitatu ziti zomwe Yuda akugwiritsa ntchito potchula Akhristu omwe akuwalemba?

Kodi mau oti “osungidwa” akutanthauza chiani?

Popeza kuti akulemba iwo amene “asungidwa” kodi izi zikutanthauza kuti pali ena omwe ayitanidwa ndi kukonedwa koma sanasungidwe mwa Yesu?

Vesi 3:

Kodi mau oti “chipulumutso cha ife tonse” akutanthauza chiani?

Kodi nchiyani chomwe chikuonetsa mu vesi 3 kuti Mzimu Woyera wapangitsa maganizo a Yuda kuti asinthe nkhani yaikulu ya kalata wake?

Kodi poyamba amafuna kulemba za chiyani?

Kodi oyera mtima omwe akunenawa ndi ati?

Vesi 4:

Chifukwa chiyani Yuda akuwachenjeza kuti alimbane chifukwa cha chikhulupiriro?

Nanga mau oti “kulimbana” akutanthauza chiyani?

Kodi ndimeyi ikuonetsa kuti aphunzitsi onyengawo ali pafupi kufika kapena afika kale?

Kodi anthu oipawa akwawira mu chiyani?

Ndi mau awiri ati omwe akufotokozera Yesu Khristu?

Ndi mau atatu ati omwe akufotokozera anthu ochimwawa?

Vesi 5-8:

Kodi ndi mfundo ziwiri ziti zokhuza Israel zomwe zatchulidwa mu vesi 5?

Kodi mfundozo zikugwirizana bwanji ndi nkhani yaikulu ya Yuda?

Kodi mngelo wamkulu yemwe akufotokozeredwa mu vesi 6?

Kodi akamati “tsiku lalikulu” akutanthauza chiyani?

Nanga “moto wosatha” ndi chiyani?

Vesi 9-10:

Kodi Mikayeli anali ndani?

Chifukwa chiyani Mikayeli sanadzudzule Mdierekezi?

Kodi nkhani yomwe inali pakati pa Mikayeli ndi Mdierekezi inali yotani?

Nanga amene akulankhula zoipa omwe atchulidwa mu vesi 10 ndi ndani?

Vesi 11:

Kodi ndi zitsanzo zitatu ziti za chilango zomwe zaperekedwa mu vesili?

Kodi tchimo la Kaini linali lotani?

Nanga tchimo la Balamu linali lotani?

Kodi tchimo la Kore linali lotani?

Kodi ndi mau atatu ati (mau ndi zochita) zomwe zikufotokozerana anthu oipa amenewa?

Vesi 12-13:

Yuda akuyerekeza anthu oipawa ndi zinthu zachilengedwe. Kodi zinthu zimenezi ndi ziti? Kodi chikufanana ndi mafunde, mitambo kapena nyenyezi ndi chiyani molingana ndi momwe akufotokozerana?

Vesi 14-16

Kodi Enoki anali ndani?

Kodi ndi chiyani chomwe munthu angayesedwe nacho kuti atamande anthu malingana ndi vesi 16?

Vesi 17-19:

Kodi chomwe chikufanana mu vesi 17 ndi mu vesi 1 ndi chiyani?

Nanga chomwe chikufanana mu vesi 17 ndi vesi 5 ndi chiyani?

Kodi mau oti “osapembedza” atchulidwa kangati mu vesi 15 ndi 18?

Vesi 20-23:

Kodi ali ndi udindo wokhala ndi chikhulupiriro malingana ndi vesi 20 ndi ndani?

Kodi mau oti “kudzimangilira” akulankhula zotani pa nkhani ya kukula msanga m’oyo wa Chikristu?

Kodi ali ndi udindo wotisunga ife m’chikondi cha Mulungu ndi ndani?

Vesi 24-25:

Kodi amene angatisunge ife kuti tisagwe ndi ndani?

Kodi kuperekedwa pamaso pa Mulungu opanda chilema kukutanthauza chiyani?

Kodi ndi zikhalidwe ziti za Mulungu zomwe zatchulidwa mu vesi 20?

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera:

2. Kodi njira ya kusanthula chaputala ndi njira yanji ya Kasanthulidwe ka Baibulo?

3. Lembani ndondomeko zinayi za kasanthulidwe ka chaputala?

(Mayankho a mafunsowa ali ku mapeto a chaputala chino)

KUPITIRIZA KUSANTHULA

1. Gwiritsani ntchito zomwe mwaphunzira mu chaputala chino kuti musanthule 2 Petro 2. Chaputala chimenechi chili ndi nkhani zofanana ndi chaputala cha Yuda chomwe tasanthula kale mu phunziro lino.
2. Gwiritsani ntchito fomu yopanda kanthu yomwe yaperekedwa m'musimu. Mutha kuchulukitsa mafomuwa kuti muwagwiritse ntchito mtsogolomu.
3. Pangani mndandanda wa mafunso kuchokera mu 2 Petro 2. Mafunsowa akuthandizani pamene mukhale mukusanthula mwatsatanetsatane ndime, mavesi ndi mau zomwe muphunzire kutsogoloku.
4. Werengani mabuku a Uthenga Wabwino: Mateyu, Marko, Luka ndi Yohani. Lembani mafunso onse omwe Yesu anafunsa ndi kuona momwe anagwiritsira ntchito mafunso popanga ena kuti aphunzire.

KUSANTHULA CHAPUTALA

BUKHU:

CHAPUTALA

MUTU WA CHAPUTALA:

Vesi

Mutu wa Ndime

Ndemanga

CHAPUTALA 11

KUSANTHULA NDIME

ZOLINGA

Pomaliza pa chaputala chino mukhala mukukwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kufotokozero momwe tinganthulire ndime
- Kusanthula ndime
- Kupanga tchati cha ndime kuti mulembe mwachidule zomwe mwapeza posanthula Mau
- Kulemba mlozo wandime ya m’Baibulo

VESI LOTSOGOLERA

Potsegulira mau anu paunikira; Kuzindikiritsa opusa. (Masalimo 119:130).

MAU OYAMBA

Mwaphunzira momwe mungachitire kafukufuku wa bukhu la m’Baibulo ndi kusanthula machaputala a m’bukhulo. Pamene mumasanthula chaputala mumachigawa m’magawo a ndime. Tsopano muphunzira kasantulidwe ka ndime. Ndipo chitsanzo cha momwe mungachitire posanthula ndime chaperekedwa. Mukhala ndi mwayi wosanthula panokha ndime mu chigawo cha “Kupitiriza Kuphunzira.”

KUSANTHULA NDIME

SITEPE 1: SANTHULANI CHAPUTALA CHONSE

Monga mwaphunzira kale, chaputala chirichonse chagawidwa m’ndime. Ndime ndi gulu la mavesi omwe akukamba nkhani imodzi. Nkhani ikusintha ndiye kuti timakhala kuti tikulowa mu ndime ina. Pamene mukusanthula chaputala, muona kuti ndime zina zikukamba nkhani yofanana. Izi nzotheke ndithu posanthula ndime.

Alumikizi

Awa ndi mau ofunikira kwambiri. Amaonetsera ubale wapakati pa ndime mu chaputala. Mau oti “koma” ndi olumikizitsa ndipo amaonetsera kuti zomwe zikubwerazi ndi zosiyana ndi zomwe zalankhulidwa kumene. Mwachitsanzo:

Koma iwowa zimene sazidziwa azicitira mwano; ndipo zimene azizindikira cibadwire, monga zamoyo zopanda nzeru, mu izi atayika, (Yuda 1:10)

Pali kusiyana kwa zinthu mu ndimeyi. Aphunzitsi onyenga amalankhula zoipa za zinthu zomwe sazidziwa KOMA amaononganso zinthu zomwe akuzidziwa. Vesi ikuyamba ndi mau oti “koma” omwe akupangitseni kuyang’ana mu vesi 9 kuti muone chomwe akusiyanitsira.

Koma Mikayeli mkulu wa angelo, pakucita makani ndi mdierekezi anatsutsana za thupi la Mose, sanalimbika mtima kumehulira cifukwa comcitira mwano, koma anati, Ambuye akudzudzule. (Yuda 1:9).

Vesi 10 ikusiyanitsa aphunzitsi onyenga omwe amalankhula zoipa za zinthu za ulemelero ndi Mikayeli mngelo wamkulu. Ngakhale kuti Mikayeli anali udindo waukulu, sanamdudzule Mdierekezi koma anati, “Ambuye akudzudzule.” Mau oti “kapena” amasiyanitsanso ndime. Mwachitsanzo:

Pakuti Mulungu adzanena mlandu wa zocita zonse, ndi zobisika zonse, ngakhale zabwino ngakhale zoipa. (Mlaliki 12:14)

Mau ena olumikizitsa ndime omwe mukuyenera kukhala nawo tcheru ndi: “monga” ndi “ngati.” M’ malo mosiyanitsa, mau awa amaonetsa kufafana kwa pakati pa zinthu. Mwachitsanzo, mu vesi liri m’ musimu Satana akuyerekezedwa ndi mkango:

Mdierekezi NGATI mkango wobuma, kuyendayenda, kufunafuna wina ukamlikhwire (1 Petro 5:8).

Mau oti “ndi” ndi mlumikizi winanso. Amaonjezera ku chomwe changolankhulidwa kumene:

Momwemonso iwo m'kulota kwao adetsa matupi ao, napeputsa ufumu, nacitira mwano maulemerero. (Yuda 1:8)

Mau oti “ngati” amatsegulira mau owonetsa kuti china chake chikuyenera kuchitika kaye china chisanachitike. Malonjezano ndi mauneneri ambiri mu Chipangano Chakale analembedwa mu

njira imeneyi. Mauwa amaonetsa zomwe Mulungu angachite NGATI (kapena kuti pokhapokha) anthu ake achite kenakake:

Ana a Manase ndiwo Asrieli amene mkazi wace anambala, Koma mkazi wace wamng'ono Maramu anabala Makiri atate wa Gileadi; (2 Mbiri 7:14)

Mau oti “kuti” amaonetsa cholinga. Amaonetsa kuti chinthu china chinachitika “ndi cholinga chakuti” china chake chikwaniritsidwe.

nadza nakhazikika m'mudzi dzina lace Nazarete kuti cikacitidwe conenedwa ndi aneneri kuti, Adzachedwa Mnazarayo. (Mateyu 2:23)

Khalaninso maso ku mau ena monga, “pakuti, chifukwa, chotero.” Mau awa amaonetsera zifukwa ndi zotsatira.

Koma Iye, poona makamuwo, anagwidwa m'mtima ndi cisoni cifukwa ca iwo, popeza anali okambululudwa ndi omwazikana, akunga nkhusa zopanda mbusa. (Mateyu 9:36)

Mau oti “mu, mwa, ndi” ndi ofunikanso. Alumikizi awa amaonetsera ubale pakati pa malingaliro.

Anasanduliza nyanja ikhale mtunda: Anaoloka mtsinje coponda pansi: Apo tinakondwera mwa Iye. (Masalimo 66:6)

Dongosolo la Kaikidwe Ka Mfundo

Pamene mukusanthula ndime, onani momwe mfundo zasanjidwira komanso momwe mavesi akuyendera limodzi. Nthawi zina wolembe atha kunena mfundo yosalunjika, kenako ndi kuifotokozera ndi zitsanzo. Nthawi zina amangopereka mndandanda wa zinthu kenako nkuomba nkota zonsezo mu mfundo imodzi. Mu chitsanzo chomwe chaperekedwa kutsogolo kwa phunziro lino, muona kuti Yuda analemba ndime zingapo pofotokera makhalidwe a aphunzitsi onyenga. Kenako, amapereka zitsanzo za m'Chipangano Chakale kuti anthu amvetse zomwe akuphunzitsa.

Kubwerezedwa kwa Mau

Liu lirilonse m'Baibulo linauziridwa ndi Mzimu Woyera. Koma ngati pali mau kapena ziganizo zomwe zabwerezedwa ndiye kuti ndi zofunika kwambiri. Mzimu Woyera amafulumizitsa anthu

olemba kuti abwereze mau ndi ziganizo zina ndi cholinga chakuti zikhazikike m’ malingaliro athu. Chitsanzo cha mau amenewa ndi akuti, “indetu, indetu.” Nthawi zonse Yesu akayamba kulankhula kwake ndi mau amenewa amakhala ngati wolengeza pamsonkhano kunena kuti, “Timverane. Pali cholengeza chofunikira kwambiri.” Santhulani mosamalitsa mau onse omwe abwerezedwa.

Mafunso ndi Mayankho

Mukuyeneranso kutchera khutu ku mafunso ndi mayankho a m’Baibulo. Nthawi zambiri olemba amatha kuyamba kulankhula nkhani pofunsa funso. Kenako afotokozera funsolo ndi kupereka yankho lako. Chitsanzo chabwino cha ichi ndi Aroma 6. Werengani chaputala chonse. Onani mafunso omwe ali mu mavesi a 1-3 ndi mayankho omwe akubweretsedwa mu chaputala chonsencho.

Mau Oyamba.

Khalani maso ku ndime zomwe zikupereka mau oyamba a mutu waukulu wa nkhani yomwe ili m’ musu mwake. Mwachitsanzo, vesi 3 ya Yuda, chaputala chomwe tasanthula kale, ikupereka mau oyamba ku ndi nkhani yotsatirayo:

Okonedwa, pakucira cangu conse cakukulemberani za cipulumutso ca ife tonse, ndafulumidwa mtima ine kukulemberani ndi kudandaulira kuti mulimbanetu cifukwa ca chikhulupiriro capatsidwa kamodzi kwa oyera mtima. (Yuda 1-3).

Ndime ya mau oyamba ngati iyi imafotokozera cholinga cha kulemba kwake. Akuwalimbikitsa kuti akhale nako kulimbana kwakukuru pa chikhulupiriro choona. Ndipo kwina konseko akufotokozera akupereka zifukwa zokhalira nako kulimbana kwakukuru pa chikhulupiriro. Pali aphunzitsi onyenga omwe akwawira mu mpingo omwe akufuna kuwatembenezira kumbali kwa chikhulupiriro choona.

Mau Owumba Nkota ndi Mau Omaliza

Khalaninso maso ku mau amene akuwumba nkota wa ndime, chaputala kapena bukhu lonse. Mwachitsanzo, bukhu la Mlaliki liri ndi vesi yomwe ikuumba nkota wa bukhu lonse. M’bukhu la Mlaliki, wolembayo akufotokozera chikhumbokhumbo chake chokhala ndi moyo wasasamala za Mulungu. Ndipo mau ake omaliza ndi akuti:

Mau atha; zonse zamveka zatha; opa Mulungu, musunge malamulo ace; pakuti coyenera anthu onse ndi ici. Pakuti Mulungu adzanena mlandu wa zocita zonse, ndi zobisika zonse, ngakhale zabwino ngakhale zoipa. (Mlaliki 12:13-14)

Kukula kwa Lingaliro

Pamene musanthula ndime, khalani maso ku kukula kwa lingaliro. Onani ndime iyi:

ndi pacodziletsa cipiriro; ndi pacipiriro zipembedzo; ndi pactpembedzo cikondi ca pa abale; ndi pacikondi ca pa abale cikondi. Pakuti izi zikakhala ndi inu, ndipo zikacuruka, zidzacita kuti musakhale aulesi kapena opanda zipatso pa cizindikiritso ca Ambuye wathu Yesu Kristu. Pakuti iye wakusowa izi ali wakhungu, wa cimbuuzi, woiwala matsukidwe ace potaya zoipa zace zakale, (2 Petro 1:6-9)

Muli kukula kwa lingaliro mu ndime imeneyi. Tikuyenera kuonjezera chinthu china ku chinzake kuti tikafikire kukubala chipatso.

Mtundu wa Kalembedwe

Iyi ndi njira yomwe wolembe amasankha kuti agwiritse ntchito polemba. Ndime zina za m’Baibulo zalembedwa mwa nkhani. Pamene ndime zina zalembedwa mwa ndakatulo kapena nyimbo monga bukhu la Masalimo. Ndime zina ndi mafanizo. Mafanizo ndi nkhani zazifupi zomwe cholinga chake chimakhala chophunzitsa kanthu kena kuzimu. Ndipo ndime zina analemba ngati sewero. Mwachitsanzo, bukhu la Nyimbo ya Solomo liri ndi ndime za sewero komanso za nyimbo. Palinso ndime zina zomwe zimalembedwa ndi cholinga chophunzitsa mutu wina wake.

Mau Ofunikira

Kuzindikira mau ofunikira mu ndime kumakuthandizani kudziwa tanthauzo la ndimeyo. Nthawi zambiri mauwa amabwerezedwa mowirikiza ndipo amakhala ndi mphamvu yaikulu pa tanthauzo la ndime. Khalani ndi chidwi makamaka ndi mau amene simukuwadziwa tanthauzo lake kwenikweni. Mutha kutenga nthawi yapadera kusanthula mau amenewa. Muphunzirabe za kasanthulidwe ka mau paokha. Werengani ndime ili m’musiyi:

YUDA, kapolo wa Yesu Kristu, ndi mbale wa Yakobo, kwa iwo oitanidwa, okonededwa mwa Mulungu Atate, ndi osungidwa ndi Yesu Kristu: Cifundo ndi

mtendere ndi cikondi zikucurukireni. Okonedwa, pakucira cangu conse cakukulemberani za cipulumutso ca ife tonse, ndafulumidwa mtima ine kukulemberani ndi kudandaulira kuti mulimbanetu cifukwa ca cikhulupiriro capatsidwa kamodzi kwa oyera mtima. Pakuti pali anthu ena anakwawira m'tseri, ndiwo amene aja adalembedwa maina ao kale, kukalandira citsutso ici, anthu osapembedza, akusandutsa cisomo ca Mulungu wathu cikhale cilak olako conyansa, nakaniza Mfumu wayekha, ndi Ambuye wathu, Yesu Kristu. (Yuda 1-4).

Kodi mukudziwa tanthauzo la mau oti “chilakolako chonyansa?” Mutha kusanthula mau awa mwapadera popeza akufotokozera za chikhalidwe cha aphunzitsi onyenga. Chimodzi mwa zikhalidwe zawo ndiko kusandutsa chisomo cha Mulungu chilakolako chonyasa. Ichi ndi chitsanzo cha mau ofunikira mu ndime kuti muwasanthule mwapadera.

Malamulo a Chiyankhulo

Chilankhulo chiri chimagawa mau osiyanasiyana molingana ndi malamulo ake. Mauwa akawalumikiza pamodzi amapanga chiganizo. Khalani maso ku mau otchedwa “aneni.” Aneni amaonetsa ntchito yomwe yachitika kale, kapena ikuchitika tsopano, kapenanso yomwe ichitike mtsogolo. Amagwiritsidwanso ntchito ngati mau aulamuliro:

MUKANI dziko lonse lapansi, ndipo MUKALALIKIRE Uthenga Wabwino kwa cholengedwa chirichonse (Marko 16:15)

Mau oti “mukani” ndi “mukalalikire” akuonetsa ntchito. Awa ndiwo aneni. Ndi mau aulamuliro kwa ife kuti tikawamvere. Mau a osonyeza maina ndi ofunikanso kwambiri kusamalitsa nawo. Awa ndi mau amene amapereka dzina kwa munthu, chinthu, kapena mal. Onani mau omwe ali mu zilembo zikuluzikulu:

YUDA, kapolo wa YESU KHRISTU, ndi m'bale wake wa YAKOBO (Yuda 1)

Mau otchula maina amaonetsa munthu kapena chinthu chomwe chatengapo mbali komanso komwe ntchitoyo yachitikira. Ndipo amlowamalo a maina amagwira ntchito m'malo mwa maina. Mau oti, “Iye” ndi chitsanzo chabwino. M'malo monena kuti, “Mzimu Woyera anauzira Yuda kuti alembe bukhuli.” Mutha kulemba kuti, “Mzimu Woyera anauzira “IYE” kuti alembe bukhuli.” Apapa mauwa agwira ntchito m'malo mwa mau oti “Yuda.”

Afotokozi ndi aonjezi ndi magawo ofunikira mu chilankhulo. Aonjezi amanena kanthu kena koonjezera pa aneni. Makamaka momwe ntchito inachitikira. Mwachitsanzo, m'chinganizo ichi, "Iye anathamanga mofulumira," mau oti "mofulumira" ndi muonjezi ndipo akuonetsera momwe munthuyo anathamangira. Mfotokozi amafotokozera dzina kapena mlowam'malo wa dzina. Tikanena kuti "Yuda ndi wantali," mau oti "wantali" ndi mfotokozi yemwe akufotokozera za Yuda.

Zinthu izi zitha kuoneka zosokoneza makamaka ngati simunaphunzirepo izi chiyambire, komano muphunzira posachedwa ngati mungamaziwerenge pafupi pafupi. Magawo a chilankhulo awa ndi ofunika chifukwa amadziwitsa malo, anthu komanso zinthu.

Amafotokozera za **yemwe** wachita, **chiyani**, **kuti**, **liti** ndi **chifukwa chiyani**. Amafotokoza momwe zinthu zinachitikira komanso kuti nchiyani chidachitika, chikuchitika, ndi chomwe chichitike mtsogolo. Amafotokozera chinthu ndi tsatanetsatane wa chinthu zomwe zimathandizira kuti munthu amvetse bwino nkhani yomwe ikukambidwayo.

SITEPE 3: KUPANGA TCHATI CHA NDIME

Posanthula ndime mwatsatanetsatane monga m'mene tafotokozera mu Sitepe 2, muona kuti ndime zina zikuyendera limodzi. Ubale wa ndimezo utha kukhala wosiyanyitsa, woyerekeza, wopitiriza ndi zina. Onani kuti kodi ubale wa ndime zomwe mukusanthula ndi wotani.

Mupanga tchatu chomwe chiumbe nkota wa zomwe mwasanthula mu ndime zimenezi. Pezani mutu waukulu wa nkhani zomwe ziri mu ndime zomwe mwasanthula. Tchatu chanucho chionetsanso mitu ya ndime ndi magawo omwe mwapanga mu nthawi yosanthula machaputala ija. Patchatipo lembani bukhu, chaputala, ndi ndime zomwe mwasanthula. Gwiritsani ntchito m'mapeto mwa tchatu chanu polemba ndemanga ndi momwe mugwiritsire ntchito zomwe mwaphunzirazo.

SITEPE 4: LEMBANI MLOZO WA NDIME

Gwiritsani ntchito tchatu kuti ikuthandizeni polemba mlozo wan dime. Milozo yomwe mwalembe posanthula machaputala ndi ndime ikuthandizani pamene mukugawana Malemba ndi ena popeza mumalankhula zinthu mwa dongosolo labwino.

CHITSANZO CHA NJIRA

SITEPE 1: SANTHULANI CHAPUTALA

Kusanthula chaputala kwachitika kale ndi pamene timasanthula Yuda 1. Pano tisanthula ndime kuchokera mu chaputala chomwechi, chotero sitepe 1 tapanga kale.

SITEPE 2: KHALANI TCHERU NDI ZOMWE ZALEMBEDWA

Pamene timasanthula ndime za Yuda 1 mwakuya, tinaona kuti ndime 4, 8-10, 16, 17-18, ndi 19 zimaonetsa ubale. Ubale wake ndi wakuti ndime zonsezi zikulankhula za makhalidwe a aphunzitsi onyenga.

SITEPE 3: PANGANI TCHATI CHA KASANTHULIDWE KA NDIME

M'mbuyomu takhala tikukupatsani tchati chokonza kale kuti mugwiritse ntchito. Koma tsopano mukuyenera kupanga tchati chanu chanu popeza nkovuta kudziwa kuti ndime yomwe mukusanthula ndi yaikulu motani komanso iri nkhani zambiri bwanji kuti zionedwe. Ichi ndiye chifukwa chimene sitinakupatsirenitutu tchati chokonza kale.

M'musimu muli chitsanzo cha Tchati cha Kusanthula Ndime. Gwiritsani ntchito chitsanzochi popanga tchati chanu chanu. Onesetsani kuti mwaika manambala a mavesi a ndime iriyonse.

Tchati cha Kusanthula Ndime

Bukhu: Yuda Chaputala: 1 Ndime: 4, 8-10, 16, 17-18, 19

Mutu: Makhalidwe a Aphunzitsi Onyenga

4

| | |
|--|--------------------------|
| Anakwawira mozemba | Mayendedwe |
| Anaikidwirani kuti akaweruzidwe kalekale | Nkhani yofunika kuidziwa |
| Amuna osapembedza | Chikhalidwe |
| Kusandutsa chisomo cha Mulungu kukhala chilakolako chonyansa | Chiphunzitso |
| Kukana Ambuye Mulungu ndi Ambuye wathu Yesu Khristu | Chiphunzitso |

8-10

| | |
|-------------------|----------|
| Olota maloto | Khalidwe |
| Odetsa matupi awo | Khalidwe |
| Apepusa ufumu | Khalidwe |

| | |
|---------------------------------------|------------|
| Nanyoza maulemelero | kulankhula |
| Achitira mwano zimene sazidziwa | kulankhula |
| Zomwe azizidziwa chibadwire aziononga | kulankhula |

16

| | |
|--|------------|
| Odandaula | kulankhula |
| Odelera | kulankhula |
| Oyenda monga mwa zilakolako zawo | kuyenda |
| Pakamwa pawo palankhula zikuluzikulu | kulankhula |
| Otama anthu chifukwa chofuna kupeza phindu | khalidwe |

18-19

| | |
|--|--------------|
| Otonza | kulankhula |
| Oyenda monga mwa zilakolako zosapembedza | mayendedwe |
| Odzipatula okha | khalidwe |
| A makhalidwe achibadwidwe | khalidwe |
| Opanda Mzimu Woyera | chiphunzitso |

Mau ofunikira kusanhula mwapadera:

Chilakolako chonyasa (ndime 4): Kodi mau awa amatanthauza chiyani?

SITEPE 4: PANGANI MLOZO WA NDIME

Mlozo wa ndime ya “Makhalidwe a Aphunzitsi Onyenga”

- I. Nkhani zawo za m’mbuyo:
 - A. Anaikidwiratu kuti akaweruzidwe.
- II. Mayendedwe awo:
 - A. Anakwawira mozemba.
 - B. Oyenda monga mwa zilakolako zawo.

- C. Oyenda monga mwa zilakolako zawo zoipa.
- III. Malankhulidwe awo:
- A. Amalankhula mwano pa zolengedwa za ulemelero.
 - B. Kulankhula zoipa za zinthu zomwe zakudziwa
 - C. Akupha.
 - D. Odandaula.
 - E. Mkwamwa mwawo modzadza mau odzitamandira.
 - F. Onyoza.
- IV. Chiphunzitsa Chawo:
- A. Kusandutsa chisomo cha Mulungu kukhala zilakolako zonyasa.
 - B. Kukana Ambuye wathu m' modzi yekhayo ndi Mpulumutsi wathu Yesu Khristu.
 - C. Alibe Mzimu.
- V. Makhalidwe awo:
- A. Osapembedza.
 - B. Olota maloto.
 - C. Odetsa thupi.
 - D. Olamulidwa ndi zilakolako.
 - E. Odzipatula okha.
 - F. Chidziwitso cha chilengedwe choipa.
 - G. Amanyozza maulamuliro.
 - H. Okondera anthu olemera okhaokha

CHAPUTALA 12
KUSANTHULA VESI
ZOLINGA

Mukamaliza chaputala chino mukhala mukukwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kufotokozera momwe mungasanthulire vesi palokha
- Kusanthula vesi
- Kulemba tchati chomwe mulembepo mwachidule pa kusanthula kwanu
- Kulemba mlozo wa kusanthula vesi.

VESI LOTSOGOLERA

Lilime langa liyimbire mau anu; Pakuti malamulo anu onse ndiwo olungama.
(Masalimo 119:172)

MAU OYAMBA

Mwaphunzira momwe mungachitire kafukufuku wa bukhu, ndi kasanthulidwe ka chaputala m’bukhumo. Mwaphunziranso za kasanthulidwe ka ndime ya mu chaputala. Mu chaputala chino muphunzira momwe mungasanthulire vesi. Chitsanzo chaperekedwa kumapeto kuti muone momwe mungasanthulire vesi panokha ndipo mupatsidwa mwayi wakuti musanthule vesi panokha. Pamene mukusanthula vesi gwiritsani ntchito zonse zomwe mwaphunzira m’mbuyomu.

KUFOTOKOZERA NJIRA

SITEPE 1: SANTHULANI VESI MOLINGANA NDI MOMWE LAGWIRITSIDWIRA NTCHITO

Vesi iliyonse ikuyenera kugwiritsidwa ntchito molinga ndi mavesi ena omwe ali pafupi nayo. Izi zimathandiza kuti mumvetse bwino uthenga womwe uli m’Mau a Mulungu. Onesetsani kuti musangotenga vesilo palokha. Mudzabwera ndi tanthauzo lolakwika. Izi ndi zomwe aphunzitsi onyenga amachita.

SITEPE 2: WERENGANI MAVESI OGWIRIZANA

Mukayamba kusanthula muona kuti pali mavesi ena omwe akugwirizana ndi vesi lomwe mukusanthulalo. Atha kumafafaniza kapena kusiyanyitsa zomwe zikukambidwazo. Nthawi zina vesi lomwe mukusanthulalo litha kumafanana ndi mavesi a m’bukhu lina la m’Baibulo. (Onani chitsanzo mu chaputala chino). Werengani ndi kusanthula mavesi amenewa.

SITEPE 3: PANGANI TCHATI CHA KUSANTHULA VESI

Sankhani mutu wa tchati chanu. Pa tchati chanucho onetsani bukhu lomwe mukusanthula, chaputala, ndi vesi. Momwe muchitire izi zitengera zomwe mwapeza nkusanthula kwanu. Ngati mumachita ntchito yomwe mumapatsidwa mu chigawo cha “Kupitiriza Kuphunzira” ndiye kuti

mutha kukwanitsa kupanga machati anu anu. Mutha kugwiritsa ntchito tchati cha mulifupi kapena mulitali kutengera zomwe mukufuna kulemba.

SITEPE 4: PANGANI MLOZO WOSANTHULIRA VESI

Pogwiritsa ntchito luso lopangira milozo lomwe mwapeza pochita ntchito zomwe mwakhala mukupatsidwa, pangani mlozo wa vesilo. Sankhani mutu woyenera, mitu ya mkati ikulu ikulu ndi ing'onoing'ono yomwe. Gwiritsani ntchito tchati yanu popanga mlozowu.

CHITSANZO CHA NJIRAYI

SITEPE 1: SANTHULANI VESI MOLINGANA NDI MOMWE LAGWIRITSIDWIRA NTCHITO

Tinasankha Yuda 1:11 kuti tionetsere momwe tingasanthulire vesi. M'mbuyomu tasanthula kale vesili molingana ndi momwe lagwiritsidwira ntchito mu chaputala ndi ndime zake. Mukasankha vesi kuti musanthule onetsetsani kuti mwamvetsa bwino momwe likugwiritsidwira ntchito mu ndime zoyandikana. Mumachita izi poona chaputala komanso ndime yomwe vesilo likupezekamo, ndipo luso lochitira izi mwaphunzira kale. Onesetsaninso kuti vesilo likugwirizana ndi zomwe bukhu lonselo likukamba. Kasanthulidwe ka Yuda 1:11 molingana ndi momwe yagwiritsidwira ntchito kaonetsedwa kale mu tchati chanu.

SITEPE 2: SANTHULANI MAVESI OGWIRIZANA NAWO

Yuda 1:11 ikugwirizana ndi mavesi ena a mu chaputala 1 okamba za aneneri onyenga. Vesi 5-7 ndi zitsanzo za mbiri ya kale ndipo vesi 12-13 ndi zitsanzo za chilengedwe za aneneri onyenga. Yuda 1:11 akugwirizananso ndi ndime zina zitatu zofunikira mu Chipangano Chakale:

Nkhani ya Kaini: Genesis 4:1-15; 1 Yohane 3:12

Nkhani ya Balamu Numeri 22-24

Nkhani ya Kore Numeri 16

Kasanthulidwe ka ndime zimenezi kalembedwa mwachidule mu tchati komanso mu mlozo.

SITEPE 3: PANGANI TCHATI CHOSANTHULIRA VESI

Onani chitsanzo cha tchati chosanthulira vesi chili m'musichi:

TCHATI YAKUSANTHULA VESI

Bukhu: Yuda Chaputala: 1 Vesi: 11

ZITSANZO ZA M'CHIPANGANO CHAKALE ZA APHUNZITSI ONYENGA Yuda 1:11: MULUNGU AKUTI: TSOKA KWA IWO

ZIFUKWA...

1. Atsata njira ya KAINI

Genesis 4:1-15: Anakana dongosolo la Mulungu kuti machimo ayenera kukhululukidwa kudzera mu kukhetsa mwanzi. Onani Ahebri 9:22 ndi 1 Yohane 3:12:

Anakantha m'bale wake popeza ntchito zake zinali zoipa.

2. Anachita mwa dyera monga kulakwa kwa BALAAM: Numbers 22-24
Anachita zinthu kuti apeze phindu la ndalama.
3. Anaonongeka mwa monga Kore: Numeri 16: Anakana utsogoleri woikidwa ndi Mulungu.

Onani momwe zikunkera zionongeka:

APITA panjira yoipa
Kenako ATHAMANGIRA zoipa mwadyera
AONONGEKA.

Zitsanzo zina za aphunzitsi onyenga mu Yuda 1:

Za mu mbiri yakale: Mavei 5-7

Zam'chilengedwe: Mavesi 12-13

SITEPE 4: KUPANGA MLOZO WA KASANTHULIDWE KA VESI:

Ichi ndi chitsanzo cha momwe mungachitire mlozo wa vesi

ZITSANZO ZA M'CHIPANGANO CHAKALE ZA APHUNZITSI ONYENGA

Bukhu: Yuda Chaputala: 1 Vesi: 11

- I. Mulungu akuti tsoka kwa iwo (aphunzitsi onyenga).
- II. Zifukwa:
 - A. Apita njira ya Kaini:
 1. Genesisi 4:1-15 – Anakana dongosolo la Mulungu la chikhululukiro cha machimo kudzera mu mwanzi.
 - a. Choonandi ichi chikupezeka mu Ahebri 9:22.
 2. 1 Yohane 3:12: Anakantha m'bale wake.
 - B. Anathamangira choipa cha Balaam chifukwa cha dyera.
 1. Numeri 22-24: Balaam anachita choipa chifukwa cha phindu
 - C. Anaonongeka monga malankhulidwe a Kore mu Chiapngano Chakale
 1. Numeri 16: Kora anakana ulamuliro wa utsogoleri wa Mulungu.
- III. Zinthu zikuyipirayipira:
 - A. Poyamba timapita njira yoipa.
 - B. Posachedwa timakhala tikusakasaka phindu.
 - C. Mapeto ake ndi kuonongeka.
- IV. Zitsanzo zina za aphunzitsi onyenga mu Yuda 1:
 - A. Zitsanzo za mu mbiri yakale: Mavesi 5-7

1. Israel
 2. Angelo
 3. Sodomu ndi Gomora
- B. Zitsanzo za chilengedwe: Mavesi 12-13
1. Mawanga a maphwando.
 2. Mitambo yopanda madzi.
 3. Mitengo yopanda zipatso.
 4. Madzi owinduka.
 5. Nyenyezi zongoyendayenda.

Kumbukirani kugwiritsa ntchito zomwe mwaphunzira mu kasanthulidwe ka vesi popeza ichi ndicho cholinga cha kusanthula vesi. Kodi vesi mwasanthulayo mungaigwiritse ntchito bwanji m'moyo kapena mu utumiki wanu. Onani gawo la “Kusanthula Mau Modzipereka” kuti mupeze njira zochitira izi.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera osonera

2. Nkofunika nthawi zonse kusanthula vesi molingaa ndi.....

3. Lembani masitepe anayi Njira ya Kasanthulidwe ka Vesi.

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto kwa bukhuli).

KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

M'maphunziro a m'mbuyomu mwachita kafukufuku wa bukhu, chaputala, ndi ndime.

Sankhani vesi kuchokera mu ndime yomwe mwaphunzira kale. Pogwiritsa ntchito luso lomwe mwapeza mu chaputala chino santhulani vesilo. Lembani zomwe mwapeza mwachidule mu tchatu chani ndi mu mlozo wanu.

TCHATI CHA KASANTHULIDWE KA VESI

MLOZO WA VESI

CHAPUTALA 13

KUSANTHULA LIU

ZOLINGA

Mukamaliza chaputala mutha kukwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kuzindikira mau ofunikira kusanthula mwapadera
- Kufotokozero momwe mungasanthulire liu palokha
- Kusanthula liu panokha

VESI LOTSOGOLERA

Pakuti indetu ndinena kwa inu, Kufikira litapitirira thambo ndi dziko, kalemba kakang'ono kamodzi kapena kansonga kace kamodzi sikadzaeokera kucilamulo, kufikira zitacidwa zonse. (Mateyu 5:18)

MAU OYAMBA

Mwaphunzira momwe mungasanthulire mabuku, machaputala, ndime, ndi ndime za m'Baibulo. Mu phunziro lino muphunzire momwe mungasanthulire ka nusu kakang'ono kwambiri ka Baibulo komwe ndi liu limodzi palokha. Chitsanzo cha momwe mungasanthulire liu chaperekedwa mu chigawo cha “Kupitiriza Kuphunzira” ku mapeto a chaputala chino.

KUTANTHAUZIRA ZINTHU

Kutanthauzira liu ndi ntchito yomwe munthu amasanthula mau a m'Baibulo. Cholinga cha kusanthula mau paokha ndi chakuti timvetse mauwo molingana ndi momwe akugwiritsidwira ntchito mu ndimeyo. Gawo lililonse la mau a Mulungu omwe ndi owuziridwa ndi ofunikira kuwamvetsa bwino.

Pakuti indetu ndinena kwa inu, Kufikira litapitirira thambo ndi dziko, kalemba kakang'ono kamodzi kapena kansonga kace kamodzi sikadzaeokera kucilamulo, kufikira zitacidwa zonse. (Mateyu 5:18)

Yesu anatchula tizilembo ting'onoting'ono kwambiri kutanthauza kuti liu liri lonse lomwe liri m'Mau a Mulungu linauziridwa ndi Mzimu Woyera. Tanthauzo la liu limathandiza kumvetsa

mavesi. Mukamvetsa bwino vesi, ndime ikhala yosavuta kuimvetsa zomwe zimathandiza kumvetsa chaputala ndi bukhu lonse.

KUFOTOKOZERA NDIME

SITEPE 1: KUSANKHA LIU LOTI MUSANTHULE

Nthawi imene timaphunzira za kasanthulidwe ka machaputala, ndime komanso mavesi tinalatchulako za mau ofunikira mundime. Awa ndi mau amene ndi tsinde la tanthauzo la vesi. Nthawi zina amakhala kuti abwerezedwa kangapo m’ndimeyo kapena ndi ovuta kuwamvetsa. Mukuyenera kukhala wosamala posankha liu loti musanthule. Mwachitsanzo, mau oti “ku” ndi “ngati” simau ofunikira kuwasanthula paokha ayi. Awa ndi alumukizi chabe ndi othandizira kukumvetsa tanthauzo.

SITEPE 2: KUSANTHULA LIU MOLINGANA NDI MOMWE LAGWIRITSIDWIRA NTCHITO

Santhulani liulo molingana ndi momwe lagwiritsidwira ntchito mu chaputala chimenecho. Kodi liulo likupezekanso mu chaputala china? Ngati likupezeka, aligwiritsa ntchito ndi tanthauzo lotani? Kodi pali vesi lina lomwe likufotokozera bwino tanthauzo la liulo? Kenako santhulani liulo molingana ndi momwe aligwiritsira ntchito mu ndime imeneyo. Kodi nkhani yaikulu mu ndime imeneyo ndi yotani? Kodi liu limene mukusanthulali likugwirizana motani ndi nkhani yaikulu yomwe iri mu ndimeyo?

Mukatero, santhulani liulo molingana ndi momwe aligwiritsira ntchito mu vesilo. Kodi ikugwirizana motani ndi vesilo? Kodi liulo liri gawo liti la magawo a malamulo a chiyankhulo? Kodi ndi dzina, mlowa’ malo wa dzina, mnene, muonjezi, kapena mfotokozi.

Yambani mwaona kaye momwe liulo lagwiritsidwira ntchito mu chaputala, ndime kapena vesi yomwe likupezeka musanayambe kulisanthula. Machaputala, ndime ndi mavesi zimagwira ntchito limodzi kutipatsa ife tanthauzo logwirika la Mau a Mulungu. Mukayamba kusanthula liu osaona kaye momwe aligwiritsira ntchito, mukhala pa ngozi yolitanthauzira molakwika.

SITEPE 3: PEZANI TANTHAUZO LA LIU

Mukasankha liu ndi kuona momwe aligwiritsira ntchito mu chaputala, ndime komanso vesilo, yesani kupeza tanthauzo lake. Khalani maso ku mau amene ndi osiyana koma okhala ndi tanthauzo lofanana, mwachitsanzo, “Ufumu wa Mulungu” ndi “Ufumu wa Kumwamba.”

Komanso mukhale maso ku mau amene ndi ofanana koma osiyana tanthauzo. Mwachitsanzo, mu Yohane 21:15-17 Yesu anafunsa Petro katatu, “Undikonda ine koposa awa?” Maulendo onse atatu Yesu anagwiritsa mau oti “chikondi” osiyana. Mutha kugwiritsa ntchito mavesi aumboni omwe amapezeka pakati pa tsamba la Baibulo lanu kuti mupeze tanthaulo leni leni la liulo poona m’mene aligwitsira ntchito mu ndime zina.

SITEPE 4: OMBANI NKOTA KUSANTHULA KWANU

Mmasitepe atatu onse omwe mwadutsa kufikira pano, mukhale mukulemba ndemanga zanu pa zomwe mukuphunzira za liulo. Lembani matanthauzo a mau omwe mukupeza mkope lanu kapena pa mbali pa ndime yomwe liulo likupezeka. Lembaninso zomwe ndime zina m’Baibulo zagwiritsira ntchito mauwo ndi matanthauzo ake.

Mukamaliza kusanthula, gwiritsani ntchito zomwe mwaphunzira pa za matchati ndi milozo kuti mulembe ndemanga zanu. Kumbukirani kulemba pa tchati kapena mlozo wanu bukhu, chaputala komanso vesi la liu lomwe mwasanthulalo.

CHITSANZO CHA KASANTHULIDWE KA LIU

SITEPE 1: KUSANKHA LIU

M’maphunziro angapo apitawo tagwiritsa ntchito Yuda 1 kuonetsera momwe tingasanthulire chaputala, ndime komanso vesi. Ndipo kuchokera nkusanthula kwathu tapeza mau oti, “chilakolako chonyansa” mu vesi 4. Mau awa ndi ofunikira kwambiri chifukwa akufotokozera chikhalidwe cha aphunzitsi onyenga omwe ndi nkhani yaikulu mu chaputala chimenechi. Chifukwa china chimene mauwa ndi ofunikira kusanthula mwapadera ndi chakuti ndi ovuta kuwamvetsa.

SITEPE 2: SANTHULANI LIU MOLINGANA NDI MOMWE LAGWIRITSIDWIRA NTCHITO.

Mwasanthula kale bukhu, chaputala komanso ndime za bukhu la Yuda. Izi zikutanthauza kuti mwadziwa kale momwe mau oti “chilakolako chonyansa” agwiritsidwira ntchito. Mwaphunzira kale kuti nkhani yaikulu m’bukhu la Yuda ndi chenjezo pa za aphunzitsi onyenga. Vesi 4 momwe mauwa akupezeka ndi imodzi mwa ndime zomwe ziri mu Yuda 1. Onani zomwe mwapeza kale posanthula chaputala ndi ndime za Yuda 1 kuti muone zimenezi.

Mu chaputala chapitachi taona za kasanthulidwe ka vesi. Simunasanthule Yuda 1:4 momwe mau oti “chilakolako chonyasa” akupezeka. Imani kaye pano ndipo musanthule vesi 4 musanapitirire ndi phunziro lino.

Mutha kuona kuti mauwa agwiritsidwa ntchito ngati mfotokozi kufotokozerera chikhalidwe cha aphunzitsi onyenga. Iwo amasanthutsa chisomo cha Mulungu kukhala chilakolako chonyasa.

SITEPE 3: PEZANI TANTHAUZO LA LIU

Mau awa amapezekanso mu mavesi otsatirawa:

Marko 7:22; 2 Akorinto 12:21; Agalatiya 5:19; 1 Petro 4:3; ndi Yuda 4. Mu ndime zonsezi mauwa ali ndi tanthauzo limodzi. Ndipo akukamba za dama, chilakolako kapena chisiliro chonyasa.

SITEPE 4: LEMBANI MWACHIDULE ZOMWE MWAPHUNZIRA

Nthawi imene timasanthula liu lakuti chilakolako chonyasa, tinapanga ndemanga pa liu limeneli. Mu sitepe yoyamba tinasankha liu loti tisanthule.

Mu sitepe 2 tinali titasanthula chaputala ndi ndime. Ndipo zinakhala mbali imodzi ya kusanthula kwathu. Munafunsidwa kuti musanthule vesi ya 4. Zomwe tinapeza nkusanthula kumeneku kukuyenera kukhala mbali imodzi ya kusanthula kwathu kwa liu.

M’musimu muli zomwe tinapeza pa nkusanthula kwathu kwa liu lakuti chilakolako chonyasa. Gwiritsani zitsanzo zimenezi kuti muumbe nkota wa zomwe mwaphunzira kuti mupange kasanthulidwe kanu kanu ka liu pogwiritsa ntchito matchati, milozo ngakhale zithunzi.

Monga tanenera kale, tikufuna kukumbutsani za kufunika kogwiritsa ntchito zomwe mwaphunzira kudzera nkusanthula liu. Kupeza nzeru pakusanthula Mau sikokwanira pakokha. Mukuyenera kukhala wochita Mau osati wongomva chabe. Mumachita izi pamene mwayamba kuchita monga mwa choonadi chomwe mwaphunzira.

KUSANTHULA LIU

Bukhu: Yuda

Chaputala: 1

Vesi: 4

Liu: Chilakolako chonyasa

Gawo la malamulo a chiyankhulo: Mfotokozi yemwe akufotokozera za makhalidwe a aphunzitsi onyenga molingana ndi Yuda 1:4.

TCHATI CHA LIU LA CHILAKOLAKO CHOIPA

| Vesi | Ndemanga |
|------------------|--|
| Marko 7:22 | Choipa chochokera mum'tima |
| 2 Akorinto 12:21 | Limodzi mwa machimo ku Akorinto |
| Agalatiya 5:19 | Limodzi mwa ntchito zathupi |
| Aefeso 4:19 | Limodzi mwa machimo a anthu osatembenuka |
| Yuda 1:4 | Chikhalidwe cha aphunzitsi onyenga |

Kupitiriza kuphunzira mau oti “chilakolako chonyansa.”

Kusanthula liu kutha kufikira ku kusanthula kwa mau and mavesi ena. Kuchokera ku kusanthula mau oti “chilakolako chonyasa” mutha kupeza mau oti ena oti musanthule.

- Santhulani mau a pa Marko 7:22 pamene aonetsa mauwa ngati tchimo lochokera mkati. ndi machimo ati ena amene amachokera mkati.
- Werenangani 2 Akorinto 2:21. Kodi ndi machimo ati ena kuphitikizapo chilakolako chonyasa omwe Paulo anawaona mu mpingo wa ku Korinto?
- Werengani Agalatiya 5:19. Kodi ndi ntchito ziti zina zathupi kupatula chilakolako choipa?
- Werengani Aefeso 4. Santhulani vesi 17-19. Pangani tchati choonetsa kusiyana kwa pakati pa anthu okhulupirira ndi osakhulupirira molingana ndi vesi 17-19 kuphatikizapo chilakolako choipa. Lembani makhalidwe a okhulupirira molingana ndi vesi 20-24.
- Santhulani 1 Petro 4:3. Kodi ndi machimo ena ati kupatula chilakolako choipa omwe ife tinkayendamo kale?
- Werengani Aroma 13:13. Kupatula chilakolako choipa ndi machimo ati ena omwe wokhulupirira sakuyenera kutenga nawo mbali?
- Santhulani chisomo cha Mulungu chomwe aphunzitsi onyenga achisandutsa kukhala chilakolako choipa. Mwachitsanzo, Tito 2:11 akunena kuti chisomo cha Mulungu

chinaonekera kwa anthu onse. Ahebri 12:15 akuonetsa kuti “tingathe kugwa mchisomo cha Mulungu.”

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera osonera.

2. Lembani masitepe anayi a kasanthulidwe ka liu limodzi m'Baibulo.

3. Kodi liu lalikulu ndi chiani mu kasanthulidwe ka liu.

4. Sankhani liu limodzi mwa mau ali m'musiwa lomwe ndi liu lalikulu lofunika kusanthula palokha.

Iye.....kudziletsa.....ngati.....ndi

(Mayankho a mafunso amenewa ali kumapeto kwa bukhu lino)

KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

Sankhani liu kuchokera mu vesi kapena ndime yomwe mwaphunzira kale m’maphunziro a m’mbuyomu. Onesetsani kuti ndi liu lalikuru kapena loti simukulimvetsa. Pangani msanthulo wa liu pogwiritsa ntchito luso lomwe mwaphunzira m’phunziro lino.

SITEPE 1: SANKHANI LIU

Liu lomwe ndasankha kuti ndisanthule ndi: _____

SITEPE 2: SANTHULANI LIULO MOGWIRIZANA NDI MOMWE LAGWIRITSIDWIRA NTCHITO MU NDIME KAPENA VESI IMENEYO.

Malemba ena ogwirizana ndi liu limeneli ndi:

SITEPE 3: PEZANI TANTHAUZO LA LIULO

Monga m’mene liu lagwiritsidwira ntchito, tanthauzo lake ndi ili:

SITEPE 4: LEMBANI MWACHIDULE ZOMWE MWAPEZA

Pangani tchati, mlozo ndi kapena chithunzithunzi choonetsa zomwe mwapeza pa liu limeneli mwachidule.

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

NJIRA ZINA ZOSANTHULIRA BAIBULO

Njira za kusanthula Baibulo mwaluso zomwe zafotokozoredwa mu bukhu lino ndi zopindulitsa koposa m'moyo komanso utumiki wanu. Komabe pali njira zina za kasanthulidwe ka Baibulo zomwe anthu akhoza kugwiritsa ntchito zomwe zaperekedwa m'chigawo chino cha zoonjezera. Ngakhale kuti njirazi ndi zosangalatsa komanso zotha kuonjezera chidziwitso chanu, njirazi si zopindulitsa kweni kweni poyerekeza ndi zija zomwe taphunzira kale. Chotero m'chigawo chino tangopereka kafotokozedwe kochepa chabe ka njirazi:

NJIRA YA NDALE:

Njirayi imagwiritsidwa ntchito posanthula nkhani zokhuzana ndi ndale za maiko a m'Baibulo. Imathandizira kumvetsa bwino momwe maiko a mu nthawi ya Baibulo amayendetsedwera. Kuti muchite mtundu uwu wa kasanthulidwe ka mau mukuyenera kupeza:

- Kupeza mtundu wa ulamuliro: wa nkhaza kapena wotsata malamulo
- Nzeru ya ulamuliro: demokalase kapena nzeru zina.
- Dera la ulamuliro:
 8. Dera lolamulidwa
 9. Magawo a deralo
 10. Maudindo a ulamulirowo
 11. Mphamvu ya dera pa ulamuliro
- Atsogoleri a ulamuliro
- Machitachita a ulamuliro
 - a. Kayendetsedwe
 - b. Zachuma
 - c. Nkhondo ndi ubale ndi maiko ena
 - d. Nkhani za malamulo
- Mphamvu ya magulu a zipembedzo pa ulamuliro wa boma
- Mphamvu ya ulamuliro wa boma nkhani yomwe mukusanthulayo

NJIRA YA MAKHALIDWE

Njira iyi imaona za chikhalidwe, machitidwe ndi maganizidwe a anthu a m’Baibulo. Imafuna kufufuza zifukwa zomwe anthu a m’Baibulo amachitira zomwe anachitazo. Zitsanzo za zomwe njira ya Kasanthulidwe ka Baibulo ka Nzeru imayang’ana ndi monga:

- XIV. Kufufuza zolinga za utumiki wa Chikristu mu Afilipi 1:14-19.
- XV. Kusanthula mphamvu ya dera la Solomo pa ulamuliro wake.
- XVI. Kusanthula zomwe Yesu anamva ngati munthu.
- XVII. Kafukufuku wa zomwe Afarisi amachita kwa Yesu ndi zifukwa zake
- XVIII. Kafukufuku wa maganizo ndi machitidwe a Eliya potha pa mpikisano wa pa Phiri la Karimeli.
- XIX. Kusanthula zolinga za anthu omwe amaletsa Nehemiya kumanganso linga la Yerusalemu.

NJIRA YA UKATSWIRI WA CHIDZIWITSO CHA ZINTHU ZAMOYO NDI ZOPANDA MOYO

Njira iyi imayan’ana kwambiri zinthu monga zomera, nyama, miyala ndi zolengedwa zina zosiyana-siyana. Kuti muchite msanthulo uwu, onani mutu womwe mukuphunzira ndi mavesi omwe akukamba zimenezo kenaka ndikuona kufunika kwake pa moyo wauzimu. Chitsanzo cha momwe kasanthulidwe aka kangaonjezere chidziwitso chanu pa Mau a Mulungu nachi:

Mutu: Mpiru (mbeu ndi chomera)

Mavesi: Mateyu 13:31; 17:20; Marko 4:31; Luka 13:19; 17:6

Phunziro lauzimu: Mbeu ya mpiru imatha kukula mwina ngati mikono itatu ndi theka. Mbeu iyi ikugwiritsidwa ntchito ndi Yesu pofuna kuyerekeza Ufumu wa Mulungu ndi chikhulupiriro. Mayambidwe opepuka a Ufumu wa Mulungu afotokozeredwa ndi fanizo la mbeu yaing’ono kwambiri. Ngakhale imayamba mochepa, kumapeto kwake imakula ndi kukhala mtengo waukuru. Umu ndi momwe Ufumu wa Mulungu umakhalira. Yesu ananenanso kuti ngati anthu angakhale ndi chikhulupiriro chaching’ono ngati kambeu ka mpiru atha kuchita zinthu zazikuru.

NJIRA YA MOYO WA TSIKU NDI TSIKU

Iyi ndi njira imene amafufuza za gulu la anthu, makhalidwe ndi maubale awo wina ndi mnzake m’gulumo. Mumayamba kusanthula mabanja, mudzi, boma ngakhale maunduna, za ntchito, mtundu wa anthu, chipembedzo, maphunziro, zotsangalatsa ndi za maluso. Chitsanzo chabwino

chitha kukhala maubale a tsiku ndi tsiku. Werengani Aefeso 5:21-6:9 ndi Akolose 3:18-4:1. Chitsanzo china gawo la azimayi mu magawo osiyanasiyana a m’Baibulo.

NJIRA YA CHIKHALIDWE CHA ANTHU

Iyi ndi njira yomwe timasanthula munthu, chilankhulo, chikhalidwe, momwe amakulira, ndi mbiri yake. Mbiri ya anthu imafufuzidwa kudzera nkukumba zinthu zomwe anthu akale amagwiritsa ntchito. Mwachitsanzo cha kusanthula chilankhulo chitha kukhala kuyerekeza zilankhulo za pa Nsanja ya Babulo (Genesisi 11) mphatso ya malilime pa tsiku la Pentekosite (Machitidwe 4). Chitsanzo cha kusanthula chikhalidwe cha anthu a m’Baibulo chitha kukhala kuona chipembedzo, luso, nyimbo, ukatswiri ndi zolembalemba za anthu a nthawi ya Baibulo. Mutha kusanthula nyimbo za ana a Israel komanso zida zawo zoyimbira zomwe zatchulidwa m’Baibulo.

KUSUNGA ZOMWE MUKUPEZA POSANTHULA MAU

Nkofunika kusunga mosamala zomwe mukupeza pamene mukusanthula Mau a Mulungu. Mwina mudzafuna kusanthula mutu womwewo, bukhu kapena ndime yomweyo nthawi ina yake. Mwina mutha kufuna kugawana ndi ena zomwe mwakhala mukuphunzira nkusanthula kwanu.

Njira yabwino yosungira zomwe mukupeza ndi kusunga mafailo a ndemanga zanu. Mutha kusunga mafailo anu molingana ndi mabuku, mitu ya nkhani, kapena maina a anthu omwe mwasanthula. Magawo atatu akulu amenewa atha kuoneka motere:

1. Mabuku: Pangani gawo lomwe muzisungiramo za mabuku omwe mukusanthula, machaputala, ndime, mavesi, mau amodzi paokha. Onesetsani kuti mukuika mwadongosolo – kuyambira Genesisi mpaka Chibvumbulutso.
2. Mitu ya Nkhani: Pamene mukusanthula mitu yosiyana-siyana, sungani moyenera. Mwachitsanzo, ngati mukuphusanthula za pemphero, ikani pamene pali nkhani zokhuzana ndi pemphero. Kaya mafanizo a Yesu, kapena maina a Mulungu, chitani chimodzi-modzi.
3. Anthu: Gawo ili likhala ndi maina a anthu osiyana-siyana omwe mwasanthula monga Mose, Davide, Yosefe ndi ena ambiri. Asanjani bwino lomwe molingana ndi maina awo.
- 4.

CHAPUTALA 14

KUSANTHULA BAIBULO POTSATA MUTU

Pamepeto pa chaputal ichi mukuyera kukwanitsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osaonera.
- Kufotokozera njira yosanthula Baibulo potsata Mutu.
- Santhulani Baibulo patsata mutu umodzi.

VESI YOTSOGOLERA:

Cifukwa cace ndikonda malamulo anu Koposa golidi, Inde golidi woyengeka, Cifukwa cace ndiyesa ngolunjika malangizo anu onse akunena zonse; Koma ndidana nazo njira zonse zonyenga. (Masalmo 119:127-128

MAU OYAMBA

Chaputala ichi chifotokozera ndondomeko yosanthula Baibulo pogwiritisa ntchito mutu. Phunziro limeneli lifotokozeredwa komanso zitsanzo ziperekedwa. Gawo la zoonjezera pophunzira likupatsani mwai oti mugwiritse ntchito zimene mwaphunzira pakusanthula Baibulo mwa inu nokha.

TANTHAUZO LA NJIRA IMENEYI

Njira imeneyi imasankha mutu umene mukufuna kusanthula mu Baibulo. Cholinga chake ndikufuna kudziwa zonse zimene Baibulo limaphunzitsa pa mutu umene tausankhawo.

KUFOTOKOZERA NJIRA IMENEYI

GAWO 1: SANKHANI MUTU:

Mukhoza kusankha mutu waukulu mu Baibulo monga zodabwitsa zonse za Baibulo. Koma mukhoza kusankha mutu waung'ono kuchokera ku mutu waukulu. Mwachitsanzo, mukhoza kusankha kuti musanthule za “zodabwitsa zimene Yesu anachita” kapena zozizwitsa zimene zikupezeka mu buku lopezeka mu Baibulo.

Poyamba mukuyenera kuchepetsa zinthu zimene mufuna kusanthula. Mwachitsanzo, mukhoza kusanthula mutu wa phunziro lanu kuchokera mu buku limodzi lopezeka mu Baibulo. Mukhoza kusankha mutu umene ukukhudza zosowa za moyo. Kapena mukhoza kusankha mutu kuchokera pa funso limene munafunsidwa koma simunathe kufotokozerana mokwanira kapena kuti mulibe chidziwitso chambiri.

Mukhoza kusankha kusanthula mitu imene mukhoza kugwiritsa ntchito pamene mukupatsa anthu ena uphungu. Mwachitsanzo, mukhoza kusankha kusanthula mutu okhudza imfa ndi cholinga choti muthe kutonthoza anthu ena. Kapena mukhoza kusankha mutu wa mantha ndi cholinga choti muthe kulimbikitsa anthu amene ali ndi mantha.

GAWO 2: SANKHANI NDIME YA M'BAIBULO:

Pamene mwasankha mutu umene mukufuna kusanthula, sankhani ndime imene mukhoza kusanthula malingana ndi mutu wanu. Mukhoza kusanthula mutu mu buku limodzi, mabuku angapo kapena mu Baibulo lonse.

GAWO 3: SONKHANITSANI ZINTHU PAMODZI:

Pezani ma vesi onse amene akugwirizana ndi mutu umene mukusanthula. Mwachitsanzo, ngati mukusanthula za zozizwitsa za Yesu, muyenera kuwerenga ma muku a Mateyu, Marko, Luka ndi Yahane. Lembani ndime ina iliyonse imene ikutchula kapena ikutchula zozizwitsa za Yesu.

GAWO 4: KOTOKOZERANI MWACHIDULE ZIMENE MWAPEZA:

Pamene mwasonkhanitsa zonse zimene mwapeza, mumakhala kuti muli ndi ma vesi ambiri. Chifukwa cha ichi mukuyenera kulondoroza bwino ndimezo kapena ma vesiwo kuti amveke.

Werengani ma vesi mwapezawo ndipo pezani mfundo zikuluzikulu. Muyenera kufunsa kuti kodi ma vesi ena akuti chiani pa nkhani yomweyi? Bweretsani ma vesi pamodzi pogwiritsa ntchito tchatu kapena kuti pofotokozerana mwachidule zimene mwapeza mu ndime zimene mwawerenga.

Kumbukirani kuti simukungofuna kudziwa zimene Baibulo limaphunzitsa, koma mukufuna kuti mugwiritse ntchito mfundo zimenezi pa moyo wanu komanso pa utumiki.

CHITSANZO CHA NJIRA IMENEYI

GAWO 1: SANKHANI MUTU

Zozizwitsa:

GAWO 2: SANKHANI NDIME YA M’BAIBULO:

Sozizwitsa mu buku la Luka:

GAWO3: BWERETSANI NDIME ZONSE PAMODZI:

Sozizwitsa mu buku la Luka: 1:11, 3:21, 4:30, 5:1, 7:11, 9:28, 10:17, 4:33, 13:11, 14:1, 17:11, 22:50

GAWO 4: FOTOKOZERANI MWACHIDULE ZIMENE MWAPEZA:

Chitsanzo chakufotokozero mwachidule:

zozizwitsa mu Buku la Luka

I zozizwitsa makumi awiri ndi ziwiri zalembedwa mu buku la Luka.

II. anthu amene anachita zozizwitsa zimenezi:

A. Mbuye wathu Yesu Khristu: 4:28-30; 4:31-37; 4:38-39; 4:40-41; 5:1-11; 5:12-15; 5:17-26; 6:6-11; 6:17-20; 7:1-10; 7:11-15; 7:21; 8:2-3; 8:22-25; 8:26-39; 8:41-42, 49, 56; 8:43-48; 9:11-17; 9:37-43; 11:14-23; 13:10-17; 14:1-6; 17:11-19; 18:35-43; 22:50-51; 24:1-7; 24:50-51.

B. Anthu ena:

1. Mngero Gabriyeli 1:11-23, 57,59
2. Mzimu Woyera 3:21-22.
3. Mulungu: 9:28-37.
4. Ophunzira: 10:17.

III. magulu a zozizwitsa:

A. Kuukitsa anthu akufa: 7:11-15; 8:41-42, 49, 56; 24:1-7

B. Kuchotsa ziwanda: 4:33-37; 8:2-3; 8:26-39; 9:14-23; 9:37-43

C. Machiritso: 4:38-39; 4:40-41; 5:12-16; 5:17-26; 6:6-10; 6:17-20; 7:1-10; 8:43-48; 13:11-17; 14:1-6; 17:11-19;18:35-43; 22:50-51.

D. Pachilengedwe: 5:1-11; 8:22-25; 9:11-17.

Chitsanzo cha kufotokozera mwachidule:

Mukhoza kufotozera zinthu mwachidule pogwirisa ntchito mndandanda komanso mitu ili munsimu:

Chozizwa: kodi ndi chozizwa chanji chatchulidwa.

Gawo lake: kodi chozizwa chimenechi chinachitika pa chilengedwe, ndi machiritso, kuukitsa akufa, kuchotsa ziwanda?

Malo: Kodi zinthu izi zinachitika mu nyengo yanji?

Anthu: kodi anthu amene akukhudzidwa ndi izi ndi ndani?

Njira: Kodi ndi njira yanji imene inagwiritsidwa ntchito? Ndi mau olankhuridwa kodi, kukhudza kapena, ndi pemphero kodi?

Zotsatira: kodi zotsatira za chozizwa chimenechi chinali chiani?

Maonedwe a anthu: Kodi anthu anazilandira izi bwanji kapena anali gawo limodzi la izi ndi ndani?

Mukhoza kugwiritsanso ntchito tchatu pofuna kufotokozera zinthu pogwiritsa ntchito chithunzi chili pansichi?

| Chozizwa | Gawo | malo | anthu | njira zotsatira | mmene anachitira: |
|-----------------|-------------|---------------------------------|---------------------------|------------------------|-----------------------------------|
| Machiritso | kuthupi | kunyumba Apongozi A petro | Petro ndi apongozi ake | kudzudzula | anadzuka ndi kutumikira anthu ena |

Chithunzi chimene chili pamwambachi chimagwiritsidwa ntchito pofuna kusanthula zozizwa.

Choncho sichingagwiritsidwe ntchito pa mitu ina, koma ndi chitsanzo chimene mukhoza kugwiritsa ntchito pofuna kusanthula mitu ina. Zina mwa zitsanzo za mmene mungagwiritsire ntchito izi pa moyo wanu komanso utumiki ndi izi: ganizirani zitsanzo zina.

- Kodi zozizwa zikuyenera kukhala gawo limodzi la utumiki wa okhulupirira? (werengani Mateyu 16:17-18: Yohane 14:12.

- Kodi mungaphunzire chiani pa zimene Yesu anaphunzitsa zokhudza ziwanda, imfa ndi matenda? Ndipo mungazigwiritse ntchito bwanji ku utumiki wanu?
- Kodi mungaphunzirepo chiani pakati pa chikhulupiriro ndi zozizwa ndipo mungazigwiritse bwanji ntchito pa moyo ndi pa utumiki wanu?
- Kodi zotsatira za zozizwa zenizeni ndi chiani? Kodi zotsatira zimenezi zitithandize bwanji pakuzindikira zizindikiro zonyenga?

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera.

2. Fotokozerani tanthauzo la Kusanthula Baibula posankha mutu.

3. Tchulani njira zinayi za kusanthula Baibulo potsata mutu?

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Pitirizani kuphunzira mutu wa zozizwa. Werengani zozizwa zonse mu buku la Mateyu.

Pangani ndandanda ofanana ndi umene waperekedwa mu chaputala ichi pa zimene mutapeze mu buku la Mateyu. Ngati mungakonde mukhoza kumaliza kusanthula buku la Luka limene linayambidwa kale mu chaputala chino. Gwiritsani ntchito tchati kuti mufotokozere zozizwa zimene mupeze. Pali zozizwa zambiri zimene zikupezeka mu Chipangano Chatsopano, choncho ngati mungakonde mukhoza kupitiriza kuwerenga ma Buku a Yohane ndi Machitidwe kuti mupitilire kusanthula zozizwa zina mma buku amenewa.

Mukhozanso kuwerenga zozizwa zina mu Chipangano Chakale. Ngati mungafune kutero, ena mwa mabuku amene mungawerenge ndi amenewa:

Genesis: 1; 19:26

Eksodo: 17

Numeri: 6

Yoswa: 3

Oweruza: 3

I ndi II Samueli: 3

I ndi II Mafumu: 26

Danieli: 2

Yoweri: 1 (Yoweri 1:17)

Yona: 1

Chozizwa mu Buku la _____

Chizizwa gawo malo anthu njira zotsatira maonedwe a anthu

CHAPUTALA 15

KUSANTHULA BAIBULO POYANG'ANIRA MOYO WA MUNTHU

ZOLINGA

Pamapeto pa phunziro ili mukuyenera kukwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osaonera.
- Kufotokoza tanthauzo la kusanthula Baibulo powona moyo wa munthu.
- Kusanthula Baibulo pawona moyo wa munthu.

VESI YOTSOGOLERA:

Koma izi zinacitika kwa iwowa monga zoticenjeza, ndipo zinalembedwa kuticenjeza ife, amene matsirizidwe a nthawi ya pansi pano adafika pa ife. (1 Akorinto 10:11)

CHIYAMBI

Chaputala ichi chifotokozera njira ya kusanthula Baibulo pakufukula moyo wa munthu. Chitizano cha njira imeneyi chiperekedwa komanso chigawo cha zoonjezera pophonzira chikupatsani mwai oti musanthule Baibulo powona moyo wa muthu.

KUFOTOKOZERA TANTHAUZO LA NJIRA IMENEYI

Iyi ndi njira imene imakhazikika pa moyo wa muthu winawake. Pakusanthula moyo wa anthu a m'Baibulo mukhoza kuphonzira kuchokera muzimene anadutsamo. Baibulo limafotokoza kuti:

Koma izi zinacitika kwa iwowa monga zoticenjeza, ndipo zinalembedwa kuticenjeza ife, amene matsirizidwe a nthawi ya pansi pano adafika pa ife. (1 Akorinto 10:11)

zinthu zimene zinachitika mu moyo wa anthu amene analembedwa mu Baibulo zinalembedwa ndi chitsogozo cha Mzimu Woyera ndi ndi cholinga choti ife tipindure. Zinthu zimene anakumana nazo tikhoza kupeza phunziro lauzimu. Pa kuona zinthu zolakwika zimene anachita, tikhoza kupewa zinthu zolakwika zauzimu. Ndipo pakuona zinthu zimene anachita bwino pa moyo wao wauzimu, tikhoza kuchita bwino nafenso.

KUFOTOKOZERA NJIRA IMENEYI.

GAWO 1: SANKHANI MUNTHU AMENE MUKUFUNA KUTI MUPHUNZIRE:

Sankhani munthu amene amakupatsani chidwi chapadera. Mukhoza kusankha mmodzi mwa anthu amene akupezeka pa Ahebri 11, Agalatiya 3:7 kapena Luka 4:27. Mukhoza kusankha munthu amene akupezeka mu buku la Baibulo limene mukuwerenga. Koma kumbukirani kuti munthu opambana wanthawi zonse amene mukhoza kusanthula ndi Yesu.

Mukuyenera kusamala kuti musasokoneze maina. Mwachitsanzo, pali a Zakariya okwani 30, a Natanieli okwana 20, a Yonatani okwana 15, a Yudasi okwana 7, a Yakobo okwana 5 ndi ena ambiri. Wonenetsetsani kuti anthu amene mwasankhawo ndi anthu amene mukuyenera kusanthula osati munthu wina amene ali ndi dzina lomwero.

Koma samalani ndi anthu amene ali ndi maina okwana awiri. Mwachitsanzo Yakobo amene dzina lake linasintha kukhala Israeli, Abramam amene dzina lake linasintha kukhala Abrahamu ndi Sarai amene dzina lake linasintha ndikukhala Sara, Suulo amene dzina lake linkhala Paulo.

GAWO 2: KUBWERETSA ZINTHU PAMODZI

Bweretsani zinthu zonse zimene mukufuna kudziwa zokhudzana ndi munthu amene mwasankha. Ngati muli ndi bukhu lathandiza kufufuza, gwiritsani ntchito bukuli. Koma ngati mulibe gwiritsanio ntchito Baibulo lanu kuti musanthule zokhudza munthu ameneyu. Nthawi zambiri mavesi okamba za munthu amene mwasankha amapezeka mu buku limene mukusanthuralo kapena mu mabuku ena otsatizana. Lembani mndandanda wa mavesi onse amene mwapeza okhudza munthu ameneyu ndipo werengani Vesi ina iliyonse imene mwapeza.

GAWO 3: SANTHULANI ZINTHU ZIMENE MWAPEZA:

Mndandanda uli pansiwu ndi wa zinthu zimene muyenera kufufuza zokhudza munthu amene mukufuna kuphunzira. Nthawi zina Baibulo silimapereka chilichonse chimene cha zinthu zimene zalembedwa munsimu koma inuyo mukuyenera kuika china chilichonse chimene mwapeza chokhudza munthu ameneyu.

Gwiritsani ntchito tchatu imene ili kumapeto wa gawo la zoonjezera pophunzira za chaputala chimenechi kuti mu unikile zimene mwapeza zokhudza munthu ameneyu.

Zithu zokhudza munthu amene mukusanthula:

- Dzina ndi tanthauzo la dzina la munthuyo.
- Abale ake: makolo ake, alongo ake, ndi ena apabanja pawo.

- Kobadwira: kumene anabadwira, kufunika kwa kubadwa kwake, zinthu zodabwitsa zimene zinachitika pakubadwa pake.
- Umwana wake.
- Malo opezekerapo: kodi nkhani ya moyo wake ikuchitika kuti?
- Amzake ndi abwenzi komanso maubwenzi ena apadera.
- Ntchito imene amagwira: kodi anali ndi udindo wanji? kodi amapeza bwanji zosowa za tsiku ndi tsiku?
- Maonekedwe ake akuthupi.
- Makhalidwe abwino.
- Makhalidwe oipa.
- Zinthu zauzimui zofunika kwambiri mmoyo wao.
 - * Kukumana kwao ndi Mulungu.
 - * Kutembenuka mtima.
 - * Kuitanidwa ku utumiki
 - * Kusintha kwakululu mmoyo wao (mwachitsanzo Saulo pa njira ya Ku damasiko)
- Imfa yawo. Kodi imfayo inachitika nthawi yanji.

GAWO 4: GWIRITSANI NTCHITO ZINTHU ZIMENE MWAPHUNZIRA:

Gwiritsani ntchito zinthu zimene mwaphunzira pa moyo ndi utumiki wanu. Mwachitsanzo: Kodi ndi makhalidwe ati abwino? Mphempheni Mulungu kuti akuze makhalidwe amenewa mmoyo wanu.

Ndi makhalidwe ati oipa? Kodi makhalidwe amenewa amaonekera mmoyo wanu? Pemphani Mulungu akuthandizeni pa zinthu zimenezi.

Lembani chiganizo chimodzi chofotokozera choonadi chachikulu chimene mwaphunzira kucholera kwa munthu ameneyu. Mwachitsanzo, kuchokera ku moyo wa Samisoni munthu akhoza kunena kuti: “kulekelera ku moyo wauzimu zotsatira zake zimakhala kulempera.

CHITSANZO CHA NJIRA IMENEYI

GAWO 1: PEZANI MUNTHU AMENE MUKUFUNA KUSANTHULA

Mfumu Saulo

GAWO 2: BWERETSANI ZINTHU PAMODZI

Nkhani ya Saulo ikupezeka pa I Samueli 9-31. Nkhani yokhudza Saulo yatengedwa kuchokera ku ndime zimenezi

GAWO 3: KUSANTHULA ZIMENE MWAPEZA

Tanthauzo la dzina

Saulo amatanthauza chopemphedwa kwa Mulungu: I Samueli 19:2.

Abale ake: makolo ake, alongo ake ndi anthu ena akwao.

Ndipo panali munthu, dzina lace ndiye Kisi, mwana wa Abiyeli, mwana wa Zerori, mwana wa Bekorati, mwana wa Afiya, mwana wa Mbenjamini, ndiye ngwazi.

Saulo anali ndi ana atatu: Yonatani, morebu

Ndipo ana a Saulo ndiwo Jonatani, ndi Isivi, ndi Malikisuwa; ndi maina a ana akazi ace ndi awa: dzina la woyamba ndiye Merabu, ndi dzina la mng'ono wace ndiye Mikala; ndi dzina la mkazi wa Sauli ndi Ahinamu mwana wa Ahimazi; ndi dzina la kazembe wa khamu lankhondo lace ndiye Abineri mwana wa Neri, mbale wace wa atate wa Sauli. Ndipo atate wa Sauli ndiye Kisi; ndipo Neri atate wa Abineri ndiye mwana wa Abiyeli.

Malo obadwira;

Baibulo silimafotokoza kumene anabadwira.

Umwana wake:

Amasamalira abulu atate ake: I Samueli 9:3.

Kokhala:

ku Yuda

Ntchito imene amagwira:

Anali mfumu ya Israeli

Maonekedwe akuthupi:

Iye anali munthu wantali kwambiri kuposa anthu ambiri aku Israeli: I Samueli 9:2,10:23

Iwo anali munthu owoneka bwino kwambiri: I Samueli 9:2.

Makhalidwe ake abwino;

Amaonetsa kukhudzika ndi anthu a ba banja lake I Samuel 9:5

Amatha kusankha zinthu: I Samuel 9:2; 10:24

Analora Mzimu kuti alamulire mtima wake I Samuel 11:6; 10:6

Odzichepetsa: anabisala pa katundu wake I Samuel 10:22

Anakana kunyonga munthu I Samuel 11

Utsogoleri: Amabweretsa limodzi anthu I Samuel 11

Anali ogwidwa ndi Mzimu I Samuel 11

Pachiyambi anali munthu omvera I Samuel 9:27

Amagwirizana ndi anthu owopa Mulungu I Samuel 11:7; 10:26

Anali olimba Mtima pamaso pa Mulungu I Samuel 10:6

Pachiyambi anali munthu odzichepetsa I Samueli 9:21

Makhalidwe osankhala bwino:

Iye amapanga zimene amaona kuti ndi zabwino osati zimene Mulungu akufuna I Samueli 13:8-13

Sanamvere, ananena bodza, anakana kuvomereza kulakwitsa kwake: I Samueli 15.

Analiritsa anthu a Mulungu I Samueli 15:35

Amakhudzika ndi zimene anthu amaganiza kuposa zimene Mulungu akufuna I Samueli 10:26,14:52.

Amasankha anthu osemphana zochika kuti akhale pafupi ndi iye kusiya anthu a Mulungu amene Mulungu anawakhudza. I Samueli 10:26, 14:52.

Anali wa mantha: I Samueli 17: 11.

Anali oweruza malinga ndi maonekedwe a zinthu: I Samueli 17:33.

Anali wa nsanje I Samueli 18:6-9

Anali ndi mtima ofuna kubwenzera I Samueli 18:11.

Anapanga upandu ndi odzodzedwa wake wa Mulungu: I Samueli 18:20-30.

Zinthu zikuluzikulu zauzimu zimene zinamuchitikira:

Kukumana kwake ndi Mulungu: I Samuel 9:15-27

Kutembenuka mtima: I Samuel 10:9

Kuitanidwa ku utumiki: I Samuel 10:1

Kisinthwa kwakukulu: I Samuel 13

Imfa: anafa mosayembekezekereka.

I Samueli 31 iye anafa ndi dzanja lake lomwe. Iye anafa ndi ana ake atatu onse tsiku limodzi pamene anali kumenya nkhondo ndi a filisiti.

GAWO 4: KUGWIRITSA NTCHITO ZIMENE MWAPHUNZIRA:

makhalidwe abwino amene ndingatsate ndi awa:

Mzimu wa ambuye atati wabwera pa ine ndikhoza kukhala munthu osinthika I Samueli 10:6.1 ndiyenera kusakasaka kudzodza kwa Mulungu.

Makhalidwe osakhala bwino: pali zinthu izi zimene Saulo anachita zimene sindikuyenera kuchita:

Mulungu amafuna atsogolera emene amakonda dzina lake. Ngakhale Saulo analephera mu dera limeneli, ineyo ndikukhumba mtakhala mtsogolera amene Mulungu amakhala pa mtima: I Samueli 13:14.

Kusamvera: kuchita chimene chikuoneka chabwino osati chimene Mulungu walamura.

Kukankhiira zolakwa zako pa anthu ena. Kusamala kwambiri zimene anthu akuganiza kusiyana ndi zimene Mulungu akuganiza.

Ndikhoza kuchita bwino ndi taunikira zinthu zonse zimene Saulo sanachite bwino ndi kuunguza moyo wanga onse.

Kuitanidwa kwa Saulo kuti akhale oyang'anira wa anthu malingana ndi maitanidwe a

Mulungu: I Samuli 10:1. Anali anthu amene anapanga iye akhale mfumu. (I Samuel 12:12-15; 10:24). Mulungu ndi amene amayenera kukhala Mfumu. ndikuyenera kukhala osamala kuti ndingayambe kulandira matamando amene akuyenera kupita kwa Mulungu ndi kusokoneza chikonzero cha Mulungu.

Ngakhale kuti Mulungu anali ndi Saulo (I Samuel 10:7, 9; 13:14), koma ufumu unamuchokera mmanja mwake. Ngakhake kutu anali atalandira uneneri okhudza kutengedwa kwa ufumu wake, koma Iye kudzodza kwake anali ali nakobe. (I Samueli 14:47). Mphatso ndi maitanidwe a Mulungu sizimachoka pamaso pa Mulungu. (I Samuel 10:7, 9; 13:14). Saulo amamvabe kulankhula kwa Mulungu pa moyo wake (I Samueli 15:1) ndipo anali kupembedza Mulungube (15:31). Koma iye anali asanalape machimo ake ndipo ufumu wake unatengedwa.

Davide anazindikira kuopsya kokhudza munthu wa Mulungu kotere kuti ndikuyenera kusamaritsa ndi izi:

Chooda chachikulu chimene ndaphunzira ndi zotsatira za kusamvera Mulungu. Izi zikufotokozeredwa mu chiganizo ichi “kumvera kuposa nsembe yopsyereza ndipo kuopsa kosamvera kukufotokozeredwa mu mau a Davide “mmene amphamvu amagwera” II Samueli II Samueli 1:19.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera.

2. Footokozerani tanthauzo la kusanthula Munthu mu Baibulo.

3. Fotokozerani njira zinayi zimene muyenera kutsata posanthula munthu wa m'baibulo.

(mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa buku ili)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Sankhani munthu wa m'Baiburo ndi kusanthula moyo wake. Gwiritsani mndanda uli munsimu kuti musanthule moyo wake komanso kusanthula moyo wa anthu ena mtsogolo.

KUSANTHULA BAIBULUO POWONA MOYO WA MUNTHU.

GAWO 1: SANKHANI MUNTHU AMENE MUKUFUNA KUSANTHULA

GAWO 2: BWERETSANI ZINTHU PAMODZI

Bweretsani pamodzi ma vesi amene akufotokozera za munthuyo.

GAWO 3: SANTHULANI ZIMENE MWAPEZA ZA MUNTHUYO

Tanthauzo la dzina la munthuyo

Abale ake: Makolo ake, alongo ake, ana ake ndi abale ena.

Malo obadwira: kufunika kwa malo amene anabadwira.

Umwana mwa munthuyo.

Kumene zinthu zambiri zinachitika

Anzake ndi abwenzi ena a munthuyo.

Ntchito imene amagwira

Maonekedwe ake akuthupi.

Makhalidwe ake abwino.

Makhalidwe ake oipa.

Zinthu zikuluzikulu zauzimu zimene zinamuchitikira.

Kukumumana kwake ndi Mulungu

Kutembenuka mtima kwake

Kuitanidwa ku utumiki.

Zinthu zovuta zimene anakumana nazo.

Imfa yake

GAWO 4: GWIRITSANI NTCHITO ZIMENE MWAPHUNZIRA

Makhalidwe a bwino amene mukhoza kukuza.

Makhalidwe oipa amene mukhoza kupewa.

Choonadi chachikulu chimene mwaphunzira:

CHAPUTALA 16

NJIRA YOSANTHULA CHIPHUNZITSO

ZOLINGA

Pamapeto pa phunziro ili mukuyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera.
- Kufotokozero njira yosanthula Baibulo payang'ana chiphunzitso.
- Kutchula magawo asanu akusanthula Baibulo posayanga'ana chiphunzitso.
- Kufotokozero mau akulu a chiphunzitso.
- Kusanthula Baibulo pogwiritsa ntchito njira imeneyi.

VESI YOTSOGOLERA

Mboni zanu nzodabwiza; Cifukwa cace moyo wanga uzisunga, (Masalmo 119:129)

Chaputala ichi chifotokozero tanthauzo la kusanthula Baibulo poyang'ana chiphunzitso. Chitsanzo chiperekedwa. Mu gawo la zoonjezera pophunzira, mupatsidwa mwai oti muthe kugwiritsa ntchito zimene mwaphunzira pa kusanthula Baibulo poyang'anira chiphunzitso.

KUFOTOKOZERO TANTHAUZO LA NJIRA

Kusanthula Baibulo kumeneku kumakhazikika pakupeza chimene Baibulo limaphunzitsa. Ndi kusanthula buku limodzi lonse kapena Baibulo lonse ndi cholinga chofuna kupeza zimene Baibulo limaphunzitsa. Mau akuti Theology amatanthauza maphunziro a za Mulungu. Mkati mwa Theology muli kuphunzira zinthu ngai Mulungu Tate, Mwana ndi Mzimu woyera. Njira yosanthula Baibulo poyang'anira chiphunzitso cholinga chake ndi kubweretsa choonadi poyera. Chiphunzitso ndi mulu wa zinthu zoti ziphunzitsidwe zokhudza gawo kapena mutu wina wake.

Kusanthula Baibulo poyang'anira chiphunzitso cha Baibulo kumakhazikika pa zimene Buku la Baibulo limaphunzita pa mutu winawake. Koma kusanthula Baibulo mwandondomeko kwambiri kumakhazikikanso pa zimene Baibulo lonse limaphunzitsa. Chiphunzitso sichimapangidwa kucholera pa vesi imodzi kapena ndime imodzi yokha ayi. Chiphunzitso chachinyengo kapena chabodza chimabwera chifukwa chongokhazikika pa vesi kapena ndime imodzi. Uwu ndi ntchitidwe umene zipembedzo zabodza zimatsata.

Pamene mukusanthula Baibulo poyang'anira chiphunzitso chake, mukhoza kugwiritsa ntchito mfundo ina ili yonse imena mwaphunzira kuchokera mu buku lonse, chaputala, ndime komanso vesi.

KUFOTOKOZERA KUSANTHULA BAIBULO POYANG'ANIRA CHIPHUNZITSO

Pali magawo anayi a akulu amene amatsatidwa posanthula Baibulo potsata ndondomeko iyi:

Mndanda uli munsiu ukuthandizani kuti musankhe mutu umene mukufuna kusanthula potsata njira imeneyi.

- I. Kusanthula chiphunzitso cha Baibulo
 - A. Chiyambi chake
 - B. Vumbulutso
 - C. Kuuziridwa
 - D. Ulamuliro
 - E. Mmene Mzimu Woyera amathandizira kumvetsetsa Baibulo.
 - F. Kumasulira
- II. Kusanthula chiphunzitso cha Mulungu Tate.
 - A. Chikhalidwe cha Mulungu Tate.
 - B. Ntchito ya Mulungu Tate.
 - C. Maina a Mulungu Tate.
 - D. Utatu wa Mulungu.
- III. Chiphunzitso cha Khristu.
 - A. Chikhalidwe cha Khristu.
 - B. Ntchito ya Khristu.
 - C. Maina a Khristu.
 - D. Chakhalidwe chake cha umulungu.
 - E. Moyo wake wakuthupi.

1. Kubadwa ndi Umwana wake.
2. Ubatizo wake.
3. Kuyesedwa.
4. Kusandurika
5. Chiphunzitso.
6. Zozizwa.
7. Mazuzo ndi imfa yake.
8. Kuuka kwa kufa.
9. Kukwera kumwamba.

F. Kubwera kachiwiri kwa Yesu.

G. Uthenga wa Messiya wa Ufumu.

H. Umulungu wa Yesu, umulungu ndi umunthu wake mwa munthu mmodzi.

I. Chiyambi chake chakale lomwe ndi Mulungu Tate.

J. Maulosi a Yesu mu Chipangano Chakale.

IV. Chiphunzitso cha Mzimu Woyera

A. Chikhalidwe cha Mzimu woyera

B. Ntchito ndi utumiki wa Mzimu Woyera

1. Mu Chipangano chakale
2. Mu Chipangano Chatsopano.
3. Mu mpingo wa lero

C. Maina a Mzimu woyera

D. Chiyambi chake cha kale lomwe ndi Mulungu Tate.

E. Umulungu wa Mzimu Woyera

F. Kusiyanyitsa Mzimu woyera mu Chipangano Chakale ndi Chatsopano.

- G. Ulosi ndi zinthu zoimira Mzimu Woyera.
 - H. Mpatso za Mzimu Woyera
 - I. Chipatso cha Mzimu woyera.
 - J. Kubatizidwa mu Mzimu Woyera.
- V. Chiphunzitso cha Angelo ndi Mulungu.
- A. Magwiridwe awo a ntchito ndi dongosolo lawo.
 - B. Maina a ngelo
 - C. Ntchito ya angelo kale, lero lino ndi mtsogolo.
- VI. Chiphunzitso cha angelo oipa amene ndi ziwanda ndi Satana.
- A. Chiyambi
 - B. Kagwiridwe ntchito ndi dongosolo.
 - C. Maina awo.
 - D. Ntchito, Kale, lero lino ndi mtsogolo.
 - E. Chiweruzo ndi mathero awo.
- VII. Chiphunzitso cha Satana
- A. Chiyambi
 - B. Kugwa kwake
 - C. Maina
 - D. Ntchito yake kale, lero ndi mtsogolo.
 - E. Chiweruzo ndi mathero ake.
- VIII. Chiphunzitso cha chiyambi cha munthu ndi chikhalidwe chake
- A. Chiyambi cha munthu
 - B. Kugwa kwa munthu
 - C. Chikhalidwe cha tchimo la munthu.

- D. Chikonzera cha Mulungu pa tchimo
- IX. Chiphunzitso cha chichipulumutso
- A. Chikonzera cha chipulumuts kuchokera pa lonjezano loyamba pa Genesis 3:15 kufikira Baibulo lonse
 - B. Chiphunzitso cha mpulumutsi, Yesu (Werengani chiphunzitso cha Khristu)
 - C. Ntchito imene Yesu anagwira
 - D. Dongosolo la chipulumutso
- X. Chiphunzitso cha Mpingo. Chimakhazikika pa zimene Baibulo limaphunzitsa zokhudza mpingo umene ndi thupi la Khristu Yesu lauzimu:
- A. Mpingo ngati thupi la Khristu Yesu
 - B. Kusiyana kwa mpingo ndi Israeli
 - C. Kayendetsedwe kwa mpingo
 - 1. Ma sakramenti.
 - 2. Dongosolo
 - 3. Maudindo
 - 4. Utimiki
 - 5. Chiphunzitso cha mpingo
- XI. Chiphunzitso cha zinthu zomariza chimene chimasanthula zinthu zimene zikuyenera kuchitika chimaliziro chisanafike.
- A. Ulosi okhudza mpingo.
 - B. Ulosi okhudza Israeli.
 - C. Ulosi okhudza mafuko za dziko lapansi onse.
 - D. Uloso ukhudza mesiya. Kubwera kwake ndikukhazikitsa Ufumu Wake.
 - E. Chiukitso cha akufa
 - F. Chiweruzo

G. Ulamuliro wa Yesu wa zaka chikwi chimodzi

H. Moyo wamuyaya wa olungama mtima onse.

GAWO 2: KUFOTOKOZERA TANTHAUZO LA CHIPHUNZITSO CHIMENE TASANKHA.

Matanthauzo a ziphunzitso aperekedwa kale mu mdandanda umene uli pamwambawu kotozo sikukufunikanso kutchulanso.

GAWO 3: SANKHANI NDIME YA M’BAIBULO IMENE MUKUFUNA KUSANTHULA.

Pangani chiganizo pa mabuku kapena buku la Baibulo limene mukufuna kusanthula. Ma buku a chipangano Chatsopano ndi abwino pochita kafukufuku wa chiphunzitso cha Baibulo. Nthawi zambiri Chipangano Chakale chimalembedwa mwa ulosi. Mabuku a Uthenga Wabwino amapereka uthenge umene munthu akhoza kuchita kafukufuku wa Baibulo.

GAWO 4: KUBWERETSA ZINTHU ZONSE PAMODZI ZOKHUDZA CHIPHUNZITSO.

Bweretsani zonse zimene mwawerenga mu chaputala, ndime kapena vesi kapena buku limene kuti mubweretse zinthu zanu pamodzi. Pamene mukuwerenga, lembani zinthu zimene mukuwerengazo.

GAWO 5: FOTOKOZERANI MWACHIDULE ZINTHU ZIMENE MWAPEZA

Fotokozerani mwachidule zinthu zimene mwapeza pamene mumasanthula Baibulo gwiritsani ntchito mdandanda umene waperekedwa pachiyambi paja ndi cholinga choti pakhale dongosolo.

CHITSANZO CHA NJIRA IMENEYI

GAWO 1; SANKANI MUTU

Chitsanzo cha mutu wa kusanthula Baibulo poyang’anira chiphunzitso ndi: chiphunzitso cha Khristu Yesu.

GAWO 2: KUFOTOKOZERA TANTHAUZO LA CHIPHUNZITSO

Chiphunzitso cha Khristu chimakhazikika pa Yesu Khristu.

GAWO 3: SANKHANI NDIMEN YOTI ISANTHULIDWE

Tisanthula chiphunzitso cha khristu mu buku la Akolose.

GAWO 4: BWERETSANI ZINTHU PAMODZI

muphunziro ili, tiwerenga mndandanda wa buku la Akolose.

Buku la Akolose

I. Chiyambi 1:1-14

A. Malonje 1:1-14

B. Mayamiko 1:3-8

C. Pemphero la Paulo kwa anthu aku Akolose 1:9-14.

II. umunthu ndi ntchito ya Yesu 1:15-23

A. Mbuye wa chilengedwe 1:15-17

B. Mbuye wampingo 1:18-19

C. Oyanjanitsa: 1:20-23

III. Paulo mtumwi oyanjanitsa 1:24-2:7

A. Mazuzo 1:24

B. Mtumiki wa zinsisi za Mulungu: 25-29

C. Khumbo la lofuna kuyanjanitsa ndi kubweretsa kukhazikika mwa Khristu Yesu 2:1-7

IV. Ulamuliro wa Yesu pa Chiphunzitso chonyenga: 2:8-3:4.

A. Mbuye wamphamvu zonse 2:8-10

B. Gwero la moyo watsopano: 2:11-14.

C. Ogonjetsa maulamuliro ndi maufumu 2:15.

D. Akolose akana khristu ngati Mulungu 2:16-3:4

1. Miyambo 2:16-17.

2. Kupembedza angelo 2:18-19.

3. Okodwa ndi za dziko lapansi 2:20-23.

4. Achikunja ndi ochita chikondando ndi dziko lapansi

V. Ulamuliro wa Yesu pa moyo wachikhritsu 3:5-4:5

- A. Kuchotsa chikhalidwe kapena moyo wakale 3:5-9.
- B. Kuvala moyo watsopano 3:10-17
- C. Nyengo yapadera: 3:18-4:6
 - 1. Kunyumba: 3: 18-21
 - 2. Ku ntchito 3:22:4:1
 - 3. Ndondomeko zina 3:23-25.

VI. malangizo omaliza 4:2-6

- A. Udindo papempero 4:2-4.
- B. Udindo pakuchitira umboni 4:5-6.

(zindikirani kuti kupatula kupanga mndanda wa wabuku mukhoza kusanthulanso ndime kapena ma vesi pamene mukusanthula chiphunzitsocho. Chifukwa cha phunziro ili lokha, tapereka chitsanzo cha mdandanda wa bulu la Akolose lokha.

Chinthu china chimene chachitika ndi chakuti tinawerenga buku la Akolose ndi kulemba vesi ili yonse imene ikukamba za Khristu yesu kenako ndi kufotokozera mwachidule

Chaputala 1

- 1.1.Dzina lake: Yesu Khristu
- 1.2.Mtendere umachokera kwa Yesu.
- 1.3.Mulungu ndi Tate wa Yesu Khristu.
- 1.4.Chikhulupiriro chili mwa Yesu.
- 1.13.Ufumu wake
- 1.14.Mwa Yesu ndiye muli chipulumutso ndi chikhulukiro cha machimo.
- 1.15.Yesu ndiye chifaniziro cha chenicheni cha Mulungu, ndi oyamba pa chilengedwe chonse.
- 1.16.Zonse zinalengedwa ndi iye.

- 1.17. Iye analipo zinthu zonse kulibe ndipo mwa iye muli zonse.
- 1.18. Yesu ndiye mutu wa mpingo umene ndi thupi la khristu lauzimu
- 1.19. Chidzalo chonse chili mwa iye.
- 1.20. Yesu anabweretsa mtendera kudzera mwazi wake.
- 1.21. Yesu anakwaniritsa kutiyanjanitsa.
- 1.22. Chiyero chidzera mwa Yesu
- 1.23. Mpingo ndi thupi lake lauzimu
- 1.24. Ngati Yesu ali mwa ife, tili ndi chiyembekezo cha ulemelero.
- 1.25. Ugwiro wathu uli mwa Yesu.
- 1.26. Ntchito zake ndi zampamvu

Chaputala 2

- 2:3 Nzeru ndi chidziwitso chonse chili mwa Yesu.
- 2:5 Yesu ndiye Maziko a chikhulupiriro chatu
- 2:6 Tikuyenera kuyenda ngati Iye.
- 2:7 Tikuyenera kukula mwa Iye.
- 2:9 Umulungu onse uli mwa Iye.
- 2:10 Yesu ndi mutu wa maulamuliro ndi mphamvu zonse.
- 2:13 Yesu watipatsa ife mdulidwe wamumtima.
- 2:14 Yesu anakwaniritsa chilamuro cha Chipangano Chakale.
- 2:15 Yesu anaweruzza maulamuliro ndi mphamvu zonse.
- 2:17 Thupi la khristu.
- 2:19 Mutu wa thupi.
- 2:20 Ngati tinafa mwa Khristu, sitili omangidwanso mwa ndi dziko lapansi.

Chaputala 3

- 3.1. Tinaukitsidwa mwa Khristu.
- 3.2. Ali kudzanja lamanja la atate.
- 3.3. Yesu ndiye moyo wathu.
- 3.4. Yesu adzaonekera ndipo tidzaonekera naye limodzi
- 3.5. Yesu anaphwanya malinga olekanitsa anthu.
- 3.6. Timasandulika mu chidziwitso cha Khristu Yesu.
- 3.7. Kukhulukilirana pakati pa abale ndi kotheka chifukwa cha Yesu Khristu.
- 3.8. Mtendere umachokera mwa Khristu.
- 3.9. Mau ake akuyenera kukhazikika mwa ife.
- 3.10. Tikuyenera kupemphera mu dzina lake.
- 3.11. Tikuyenera kupanga zonse mu dzina lake.
- 3.12. Tikuyenera kutumikira Ambuye Yesu Khristu.

Chaputatala 4

4.3. Chinsinsi cha Khristu (uthenga Wabwino)

GAWO 4: KUFOTOKOZERA MWACHIDULE ZIMENE MWAPEZA.

Pogwiritsa ntchito ndandanda, santhulani zimene mwapeza powerenga buku la Akolose pa chiphunzitso cha Khristu.

Kusanthula chiphunzitso cha Khristu Ku Akolose

- I. Maina a Yesu.
 - A. Yesu Khristu 1:1
 - B. Mbuye Yesu Khristu 1:3.
 - C. Mutu wa thupi. 1:18,24
 - D. Mwana wachikondi 1:18,24
 - E. Mbuye Khristu

II. Chikhalidwe cha Yesu Khristu.

- A. Amadziwa chinachilichonse. (mwa iye muli chidziwitso ndi mzeru yonse) 2:3.
- B. Ndi wachikondi: ayanjanitsa anthu onse ndi mwazi wake chifukwa cha chikondi pa munthu: 1:20.
- C. Chiyero: ndi wangwiro: 1:29.
- D. Amapezeka penapaliponse: iye ali mwa onse: 3:11.
- E. Alibe chiyambi ndi malire: analipo zonse zisanalengedwe: 3:11.
- F. Ndi wamphamvu zonse
 - 1. Zinthu zonse zinalengedwa ndi iye: 1:16.
 - 2. Zinthu zonse zimangirika mwa iye: 1:17.
 - 3. Mphamvu ndi ulamuliro onse uli mwa iye: 2:10.
- G. Mlengi 1:16
- H. Okhululukira: 2:13
- I. Mtendendere: 1:2.
- J. Chikhulupiriro 1:4
- K. Mzeru ndi chikhulupiriro 2:2-3.

III. Umulungu wa Yesu. Anali Mulungu kuthupi.

- A. Ubale wake ndi Mulungu.
 - 1. Mwana wa Mulungu 1:3,13.
 - 2. Anapangidwa muchifaniziro cha Mulungu 1:15.
 - 3. Mwa Iye muli umulungu onse 1:19:2:9.
- B. Ntchito zake:
 - 1. Olenga 1:16
 - 2. Ogwirizitsa zinthu zonse. 1:17.

3. Mpulumutsi wa anthu onse 1:14, 20, 22; 2:13,14.
4. Oweruza maulamuliro ndi mphamvu 2:15.

C. Udindo wake

1. Mutu wamphamvu ndi ulamuliro onse.
2. Maziko a chikhulupiriro cha akhristu 1:4, 2:5.
3. Chifukwa cha utumiki pa okhulupirira.
4. Mkhala pakati olumikizikitsa munthu ndi Mulungu 3:17.
5. Mutu wa mpingo ndi thupi lake 1:24; 2:17, 19.
6. Okhala pa dzanja lamanja la Mulungu 1:24; 2:17, 19.
7. Iye ndi zonse 3:11.

IV. Umunthu wa Yesu: ngakhale anali Mulungu koma iye anali kuthupi ndipo anakhala pakati pa anthu, ndipo amakumana ndi zowawa zonse zimene munthu amakumana nazo. Koma iye anakakhala opadanda tchimo.

A. Iye anakhetsa mwazi wake 1:20.

B. Anafa 2:2:15.

C. Anaukitsidwa kwakufa 2:15; 1:18

V. Imfa yake

A. Anakwaniritsa chilamuro 2:15.

B. Anabweretsa chiweruzo pa mphamvu ndi maulamuliro onse 2:15.

C. Anayanjanitsa ndi kubweretsa mtendere pa anthu onse 1:20,22.

D. Anabweretsa chikhulukiro cha machimo 2:13,3:13.

VI. Chikukitso chake.

A. Ndi oyamba kudzuka kwa kufa 1:18.

B. Anatsikimizira chiukitso chathu 3:1.

VII. Kubwera kwake: adzaonekera mtsogolo pachimariziro cha nthawi pamene tidzaonekera pamodzi naye. 3:4.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Matanthauzo a Mau osiyanasiyana afotokozeredwa mu Chaputala ichi. Ndi zofunika kuti mudziwe matanthauzo amenewa.

Werengani mndandanda wa matanthauzo a mawu umene ukupezeka mu gawo 1. Kenako werenganinso matanthauzo amene akupezeka mu gawo 2. Sankhani tanthauzo limene likufotokozerama amene alembedwa mu gawo 1. Lembani nambala ya tanthauzo pa mpata umene waperekedwa.

Gawo 1:

Gawo 2

- | | |
|------------------|--|
| ___ angelo | 1. Maphunziro a chiphunzitso cha Baibulo a Angelo |
| ___ziwanda | 2. Maphunziro a chiphunzitso cha Yesu Khristu |
| ___Chipulumutso | 3. Maphunziro a chiphunzitso cha mpingo |
| ___Mpingo | 4. Maphunziro a chiphunzitso cha chimaliziro nthawi. |
| ___Yesu | 5. Maphunziro chiphunzitso Yesu. |
| ___Angero abwino | 6. Maphunziro a chiphunzitso cha munthu. |
| ___umunthu | 7. Maphunziro a chiphunzitso cha angero abwino. |
| ___ Satana | 8. Maphunziro a chiphunzitso cha angelo oipa amene ndi ziwanda ndi Satana. |
| Mzimu Woyera | 9. Maphunziro a chiphunzitso cha Satana. |

2. Lembani vesi yotsogolera osaonera

3. Kodi kusanthula Baibulo Poyang'anira chiphunzitso ndi chiani?

4. Tchulani magawo anayi akusanthula Baibulo poyang'anira chiphunzitso

5. Fotokozani tanthauzo la mau oti chiphunzitso

(mayanko amafunso awa ali kumapeto kwa buku ili)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Chiphunzitso cha chimariziro chimakhudza zinthu zimene zidzachitike kumapeto kwa zinthu zonse. Buku la 1 Atelasonika ndi II Atesalonika limakonetsa zinthu zimene zikuyenera kuchitika pa mapeto pa zinthu zonse. Chiphunzitso chimenechi chimakhazikika pa zakubweranso kwa Yesu kumene kumatchedwa kuti mkwaturu.

Mkwaturu udzachitika mtsogolo pamene Yesu adzabwere kudzalandira okhulupirira onse. Okhulupirira onse amene anamwalira adzaukitsidwa ndi kukakumana ndi Yesu. Ndi okhulupirira amayo adzakwaturidwa pamodzi ndi akufa ndi kukayanjanitsidwa ndi Yesu.

Pogwiritsa ntchito chitsanzo chimene chaperekedwa mu chaputala chino, santhulani Baibulo poyang'anira chiphunzitso cha buku la I ndi II Atesalonika. Bweretsani pamodzi chiphunzitso mmabuku amenewa chokhudza chimaliziro makamaka kubweranso kachiwiri kwa Yesu.

GAWO 1: SANKHANI MUTU WA CHIPHUNZITSO

GAWO 2: FOTOKOZERANI TANTAUZO LA CHIPHUNZITSO.

GAWO 3 SAKHANI NDIME ZIMENE ZA M'BAIBULO ZOTI MUSANTHULE

GAWO 4: BWERETSANI ZINTHU/ MA VESI OKHUDZA CHIPHUNZITSO
PAMODZI

GAWO 5: FOTOKOZERANI ZINTHU ZONSE ZIMENE MWAPEZA
MWACHIDULE.

CHAPUTALA 17

KUSANTHULA MA BUKU A NDAKATULO M'BAIBULO

ZOLINGA

Pamapeto pa phunziro ili mukuyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osaonera.
- Kupeza kakonzedwa kosiyanasiya ka zolembedwa za ndakaturu m'baibulo.
- Kupeza mitundu ya zolemba za ndakatulo mu Baibulo.
- Kusanthula ndakatulo m'baibulo.

VESI YOTSOGOLERA:

Ndikulemekezani kasanu ndi kawiri, tsiku limodzi, Cifukwa ca maweruzo anu alungama. (Masalmo 119:164)

Mu Baibulo muli mabuku okwana 66 amene ali ndi mbiri, ndakatulo, chikondi kungotchula zochepe chabe. Baibulo ndi buku limene muli luso la zolembalemba lalikulu. Pamene mukusanthula zinthu zimene zikupezeka mu buku la Baibulo, mumakhalanso mukusanthula uthenga wa Bukulo. Mukhoza kuphunzira zinthu zozama zauzimu zimene zimavumbulutsidwa kucholera mu bukulo. Pamene mukusanthula mapangidwe a buku, mumakhala kuti mukuunguza mmene buku linabweretsedwera pamodzi. Magawo ambiri a Baibulo amafotokoza nkhani zimene zimanetsera choonadi cha Mulungu ndipo izi zimakhala zosavuta kumvetsa. Koma mabuku asanu a Chipangano Chakale amene ndi mabuku a Miyambo, Yobu, Mlariki, Nyimbo ya Solomo ndi Masalimo analembedwa mwa ndakatulo. pali ma buku ena amene ndi zidutswa za ndakaturu ngakhale kuti mabukuwo Sali mu gawo la mabuku a ndakatulo. Mwachitsanzo, mu mabuku a Chilamuro ndi ulosi ndakaturu zimapezekamonso.

Zolembedwa za ndakaturu zofotokozeru choodani cha Mulungu ndi zosiyana ndi zolembedwa zina monga nkhani zopezeka mu Baibulo. Komanso ndakaturu za m'baibulo ndi zosiyana kwambiri ndi ndakaturu zimene tonse timazidziwa. Chifukwa cha ichi, ndondomeko zapadera zoperekedwa kuti zikuthandizeni kuti musanthule mabuku amenewa.

Chaputala chimenechi chifotokoza kakonzedwe ndi mitundu ya zolembedwa za ndakatulo mu Baibulo. Chidziwitso cha zinthu izi chikuthandizani kuti muthe kugwiritsa ntchito choonadi chazimu chopezeka mu Mabuku a ndakaturu m'baiburo.

KAKONZEDWE KWA NDAKATULO

Ndakaturu za Baibulo ndi zosiyana ndi ndakaturu zimene mukuzidziwa. Ndakaturu za Baiburo zinalembedwa mu ndakaturu za chiheberi chifukwa chakuti chipangano chakale chinalembedwa mu chiheberi. Mfundo yaikulu ya ndakaturu za m'baibulo ndi yakuti zonse zimakhala ndi mau ofananirako kapena kuti ofanana. Mwachitsanzo, mizere iwiri ili pansipayi ndi yofanana.

Ndakaturu za chiheberi zimakhala ndi maganizo kapena kuti mfundo zofanana. Mzere wina uli onse wa ndakatulo umakhala ndi ganizo kapena kuti mfundo imene imakhala yogwirizana ndi mfundo inzake yopezeka pa mzere wina wa ndakaturuoyo.

Pali kufanana kunayi kumene kumagwiritsidwa ntchito mu ndakaturu za chiheberi:

1. KUFANANA KOBWEREZA

Yehova! Ha! acuruka nanga akundisautsa ine! Akundiukira ine ndi ambiri.

(Masalmo 3:1)

Wokhala m'mwambayo adzaseka; Ambuye adzawanyoza. (Masalmo 2:4)

Mu zitsanzo ziwiri zonse zimene zaperekedwa, nzere wachiwiri ukungofotokoza mfundo imene yafotokozeredwa kale mu mzere oyamba pogwiritsa ntchito mau ena chabe. Ganizo limene lafotokozeredwa mu mzere wachiwiri limakhala lofanana ndi ganizo la mzere oyamba.

2. KUFANANA KOTSUTSANA

Mu ndakaturu zimenezi, ganizo la mzere wachiwiri wa ndakaturu limakhala lotsutsana ndi ganizo la mzere oyamba. Koma mizere iwiri yonse imakhalabe yofanana chifukwa chakuti pamakhala kuti pali choonadi chimodzi chimene chikukambidwa. Ndakaturu zimenezi zimagwiritsa ntchito mau otsutsana pofuna kufotokoza choonadi. Ichi ndi chifukwa chake zimatchedwa ndakaturu zofanana motsutsana.

Chitsanzo:

Pakuti Yehova adziwa mayendedwe a olungama; Koma mayendedwe a oipa adzatayika. (Masalmo 1:6)

Mu ndakaturu imeneyi, ganizo la mzere oyamba ndi lotsutsana ndi ganizo la mzere wachiwiri. Mzere oyamba ukukamba za njira ya munthu wangiwo pamene mzere wachiwiri ukukamba za njira ya munthu opanda ungiwo. Koma mzere oyamba ndi ofanana ndi mzere wachiwiri chifukwa chakuti ukugwirizana ndi zimene zafotokozeredwa mu mzere oyamba popereka choodani chosiyana.

3. KUFANANA KOPITILIRA

Izi ndi ndakaturu zimene zimakhala ngati munthu akumanga ndi njerwa. Mzere wachiwiri ndi mizere ina yonse ya muni imakhala ikupitiriza kukuza ganizo limene laperekedwa mzere oyamba. Onani chitsanzo chimene chaperekedwa pansipa. Ganizo la mzere wachiwiri ndi mizere ina yonse imene ili muni ikuonjezera kufotokozerana zimene zakambidwa kale mu mzere oyamba:

WODALA munthuyo wosayenda mu upungu wa oipa, Kapena wosaimirira m'njira ya ocimwa, Kapena wosakhala pansipa pa bwalo la onyoza. Komatu m'cilamulo ca Yehova muli cikondwerero cace; Ndipo m'cilamulo cace amalingima usana ndi usiku. (Masalmo 1:1-2)

Pa vesi yoyamba akutu munthu ameneyu ndi odala ngati sayenda mu upungu wa oipa. Mzere umene ukubwera muni ukuonjezera pa mfundo imene yakambidwa pa mzere oyamba ponena kuti iye samaimanso pa njira ya oipa. Vesi 2 pa mzere oyamba ikufotokoza kuti iye akondwera mu chilamuro cha Mulungu. Mzere wachiwiri ukuonjezera pa mfundo yoti iye alingalira mau a Mulungu nthawi zonse.

4. KUFANANA KWA CHIZINDIKIRO

Chizindikiro ndi chinthu chimene chimaimira chinthu china kapena kusonyezera zinthu zina. Mwachitsanzo, Nyenyezi zimene zimapezeka pa mbendera ya Amerika zimaimira maboma onse amene ndi gawo limodzi la gwiranzano wa dziko la Amerika. Mu ndakaturu za kufanana kwa chizindikiro, mzere wa chiwiri ndi mizere ina yotsatira imakhala chizindikiro kapena imaonetsera za mzere oyamba.

Chitsanzo:

Ndidzayamika Yehova ndi mtima wanga wonse; Ndidzawerengera zodabwiza zanu zonse. (Masalmo 9:1)

Mzere wachiwiri mu vesi imeneyi ikuonetsera kapena kuimira mzere oyamba. Mfumu Davite okuonetsera moyo wake ukufunafuna Mulungu ngati mmene nswala ifunira madzi ikakhala ndi ludzu. Chitsanzo cha nswala ndi chizindikiro chimene chikuonetsera ludzu lauzimu la Davide. Ngakhale kuti pali zitsanzo zingapo zamitundu ya ndakaturu za chiheberi koma mitundu inayo simapezekapezeka mu Baibulo kotero kuti sikuyenera kufotokozero mu phunziro limeneli.

KUGWIRITSA NTCHITO KAKONZEDWE KUTI MUMVETSE ZIMENE ZIKUPHUNZITSIDWA

Kuzindikira kakonzedwa ka ndakaturu ndi kofunika pamene mukutanthauzira Baibulo. Izi zimakutanthandizani kuti mumvetsetse zimene zalembedwa.

1. Mau obwerezedwa.

Mu ndakaturu za chihebri kubwerezabweza kwa mau kumachitika ndi cholinga chakuti choodani chikhazikike pamtima pa munthu. Izi zimathandizira kuti kulingalira mau a Mulungu mosavuta. Mwina mkutheka kuti simunamvetse mfundo ina mu vesi ina, koma chifukwa chakubwereza zimathandiza kuti muthe kumvetsetse chifukwa chakuti mizere ina imafotokozero choonadi chomwecho.

2. Ziganizo zotsutsana koma choonadi chimodzi

Kudzera mu kakonzedwe kameneka, zimathandiza kuti musangophunzira choonadi chokha, komanso kuti mudziwe chotsutsana chofanana ndi choonadi. Chitsanzo cha izi ndi Salimo 1:6. Simumangophunzira za choonadi cha mmene munthu wangwiro amachitira komanso taonanso mmene munthu oipa amachitira. Izi zithandiza kuti tisangowiritisa ntchito choonadi chabwino chokha pamoyo wathu komanso timachenjezedwa za kuopsya kwa choonadi chosemphana. Muchitsanzo chimene tagwiritsa ntchito, taona kuti Mulungu amadzidwa njira zathu ngati tili anthu olungama. Ndipo ichi ndi choonadi chabwino. Taonanso kuti munthu osalungama mathero ake ndi chionongeko.

3. Choonadi chopitilira

Pamene mzere uli onse wa ndakaturu ukuonjezera zimene zakambidwa kale, izi zimathandiza kuti choonadi chikhazikike mu mtima.

4. Chizindikiro choonetsera choonadi cha Mulungu.

Chitsanzo chimenechi chimapereka chithunzithunzi cha choonadi cha Mulungu m'maganizo athu.

MITUNDU YA NDAKATULO

Pali mitundu itatu ya ndakaturu za chiheberi. Ndakaturu zimenezi zimasiyanitsidwa malingana ndi zimene zikupezeka mu ndakatururomo kapena mmene ndakaturuoyo yafotokozeredwa kapena kulembedwera. Ngati mungathe kuzindikira ndakaturu zosiyanasiya za m'Baibulo, izi zikuthandizani kuti mumvetse zinthu zimene mukuwerenga. Mitundu itatu ya ndakaturu ndi iyi:

1. NDAKATULO ZITALI ZITALI

Izi ndi ndakaturu zimene zimafotokozera nkhani zitali zitali za mchitidwe odzipereka kwa munthu. Ndakaturu zofotokozeredwa nkhani zimapezeka apo ndi apo mu Baibulo. Werengani Numeri 22 mpaka 24. Iyi ndi nkhani ya Balamu ndipo ndi chitsanzo cha ndakaturu zitali zitali zolembedwa ngati nkhani.

2. NDAKATURO ZAZISUDZO

Izi ndi ndakaturu zimene zimalembedwa mwachisudzo. Buku la Yobu ndi chitsanzo chabwino cha ndakaturu za chisudzo. Pachiyambi pa nkhanipo tikupatsidwa mwayi kuti tithe kuona zinthu zimene ndi zosaonekera kwa anthu ambiri. Kenako tikupeza anthenga akufotokozera Yobu mavuto amene amugwera makamaka imfa ya ana ake ndikuonongeka kwa chuma chake. Ndipo kenako tikuona Yobu ali yekhayekha pa mulu wa phulusa. Mu magawo ena a nkhani imeneyi tikupeza kuti anzake a Yobu akufotokozera zifukwa zimene Yobu akukumana ndi mavuto. Pa chimake pa nkhaniyi ndi pamene Yesu akumva mau kuchokera kwa Mulungu ndipo iye pamapeto pake akubwenzeretsedwa madalitso ake onse akuthupi. Buku la Yobu ndi ndakaturu imene ukufotokozeredwa mwachisudzo.

3. NDAKATULO ZOIMBA NYIMBO

Izi ndi ndakaturu zimene zimaimbidwa nyimbo. Zitsanzo zabwino ziwiri zikupeze mu nyimbo ya Debora mu buku la Oweruza chaputala 5 komanso nyimbo ya Miriyamu pa Eksodo 15. Palinso

magawo ena ndakatulo za nyimbo zimene zimagwiritsidwa ntchito pachisoni kapena pamene akulira maliro. Zitsanzo za izi zikupezeka pa Salimo 137,74,80 ndi II Samueli 1:19: -27. Buku la maliro ndi chitanzo chabwino cha ndakaturu zimenezi. Buku lineneli linalembedwa mwa ndakaturu ngakhale kuti limapezeka ku gawo la mabuku a mbiri. Izi zili chomwechi chifukwa chakuti ndakatulo zimenezi zimafotokozera nsautso umene anthu a Mulungu anakumana nao.

MABUKU A NDAKATULO: KUPITILIRA KWA MOYO WA UZIMU.

Mabuku asanu a ndakatulo amaonetsa kupitilira kwa moyo wauzimu. Buku la Yohane amaonetsera imfa ya moyo wakale. Masalimo amaonetsera moyo watsopano mwa Mulungu kudzera mu zinthu ngati matamando, pemphero, kupembedzera ndi kulambira. Buku la Miyambo limatitengera mkalasi kuti tiphunzire zinthu zakumwamba koma zoti tikhoza kugwiritsa ntchito pa dziko lapansi. Buku la Mlaliki limakamba zakutsata zinthu zachabechabe pa dziko lapansi. Pamene Buku la Nyimbo ya Solomo limakamba zakukhala ndi ubale ndi Yesu Khristu.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

Lembani Vesi yotsogolera osaonera.

Yang'ani ndanda 1 umene ukutchula mitundu ya ndakatulo za m'baibulo. Werengani mndandanda 2 umene ukufotokozera tanthauzo la mtundu wa ndakatulo. Lembani chilembo cholondola pa mpata chimene chikufotokozera mtundu wa ndakatulo imene yalembedwayo.

- | | |
|--------------------------|---|
| ___ ndakatulo zachisudzo | a. ndakatulo zimene zimaimbidwa. |
| ___ Ndakatulo za nkhani | b. ndakatulo za chisudzo. |
| ___ ndakaturu za nyimbo | c. ndakaturu zimene zimafotokozera nkhani komanso kuonetsera kulimba mtima kwa munthu |

Werengani mdandanda 1 pa kakonzedwe kosiyasiyana ka ndakatulo za Baibulo. Kenako werengani mdandanda 2 umene uli ndi tanthauzo la kakonzedwa ka ndakatulo za Baibulo ndipo lembani chilemba chimene chikufotokozera tanthauzo loyenera la kakonzedwe ka ndakatulo.

- | Mdandanda 1 | mdanda 2 |
|-----------------------------|---|
| ___ Kufanana kobwereza | a. mzere wachiwiri ndi mizere ina yotsatira imapereka chizindikiro kapana chitsanzo pofuna kufotokozera choonadi cha mzere oyamba. |
| ___ Kufana kwa chizindikiro | b. mzere wachiwiri ndi mizere ina yotsatira imapereka choonadi chotsutsana chimene chimagwirizana ndi mfundo ya mzere oyamba |
| kufanana kotsutsana. | C. mzere wachiwiri ndi mizere yonse yotsatira imafotokozera mfundo yotsutsana ndi mzere |

oyamba.

_____ kufanana kopitilira

D. mzere wachiri ndi mizere yonse imakhala ndi
choodani ndi chofanana ndi choonadai chimene
chafotokozeredwa mumzere wachiwiri.

4. Werengani Salimo 3:1Ndime imeneyi inalembedwa ndi kufanana _____

5. Werengani Salimo 1:6 ndime imeneyi inalembedwa ndikufanana _____

6. Werengani Salimo 1:1-2 vesi imeneyi inalembedwa ndi kufanana _____

7. Werengani Salimo 42:1 Vesi imeneyi inalembedwa ndi kufanana _____

(mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa buku ili)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Kupatula mabuku a ndakatulo, pali magawo opezeka patalipatali mu Chipangano Chakale ndi Chatsopano. Zina mwa ndime zimenezi ndi izi:

| | |
|----------------------|------------------------------------|
| Genesis 4:23-24 | Lameki kuimbira azikazi ake. |
| Eksodo 15:1-21 | Nyimbo ya Mose ndi Miriyamy |
| Numeri 21:27-30 | Nyimbo ya alakatuli |
| Numeri 23:7-10 | Nyimbo ya Balamu |
| Deteronome 33:1-47 | Nyimbo ya Mose |
| Yoswa 10:12-14 | Nyimbo ya Yoswa |
| Oweruza 5:1-31 | Nyimbo ya Debora |
| Rute 1:16-17 | Nyimbo ya Rute |
| I Samueli 2:1-10 | Nyimbo ya Hana |
| II Samueli 3:33-34 | kulira kwa David kulira Abina |
| II Samueli 1:17-27 | Nyimbo ya Saulo ndi Yonatani |
| II Samueli 22:2-51 | Nyimbo ya Davide ya chigonjetso |
| II Samueli 23:1-7 | Mau a Davide amariza |
| I Mbiri 16:8-36 | Kuyamika kwa davide |
| Yeremiya 9:17-22 | Kulilira dziko logonjetsedwa |
| Maliro 1,2,3,4,5 | Kulilira dziko logonjetsedwa |
| Ezekieli 27:25-28:23 | Ulosi otsutsana ndi mzinda wa Taya |
| Ezekieli 19:1-14 | Kulilira atsogolera a Israeli |
| Hoseya 2:1-15 | Nyimo yachidzudzulo cha Israeli |
| Habakuku 3:1-19 | Pemphero la Habakuku |
| Luka 1:46-55 | Nyimbo ya Mariya |

Luka 1:68-79

Nyimbo ya Zakariya

Luka 2:29-32

madalitso a Simiyoni

CHAPUTALA 18

KUSANTHULA ULOSI WA M'BAIBULO

ZOLINGA

Pamapeto pa chaputala ichi mukuyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osaonera.
- Kutchula kufunika kutatu kophunzira ulosi wa Baibulo.
- Kufotozera ma gwero atatu a ulosi wa Baibulo.
- Kufotokozero tanthauzo la ulosi wa Baibulo.
- Kutchula njira ziwiri zimene Mulungu amaperekera ulosi.
- Kusiyanitsa pakati pa ulosi wabodza ndi ulosi weniweni.
- Kutchula zolinga zitatu za ulosi.
- Kutchula nsanamira zisanu zothandiza kumvetsa Baibulo.

VESI YOTSGOLERA

Ndipo anati kwa iwo, 5 Awa ndi mauwo ndinalankhula nanu, paja ndinakhala ndi inu, kuti ziyenera kukwanitsidwa zonse zolembedwa za Ine m'cilamulo ca 6 Mose, ndi aneneri, ndi masalmo. (Luka 24:44)

Tinakamba kale muphunziro ili kuti pali mabuku angapo amene amatchedwa mabuku a ulosi. Chaputala ichi chifotokozero ndondomeko zothandiza kumvetsa ulosi wa Baibulo.

MABUKU A ULOSOI

Mau a Mulungu amene ndi Baibulo ndi osiyana kwambiri ndi zolembedwa za zipembedzo zina. Koma pali kusiyana kwakukulu pakati pa Baibulo ndi mabuku ena. Kusiyana kumeneku ndi kwakuti Baibulo liri ndi maulosi amene anakwaniritsidwa pamene mabuku ena alibe zimenezi. Kukwaniritsidwa kwa maulosi opezeka m'baibulo ndi chizindikiro choti Baibulo ndi Mau a Mulungu owuziridwa.

TANTHAUZO LA ULOSI

Mau oti ulosi amatanthauza kubweretsa zinthu poyera. Ulosi wa Baibulo umabwera motere:

1. Uthenga ochokera kwa Mulungu.
2. Kulosera zinthu zochitika mtsogolo muchikonzero cha Mulungu.
3. Muthu kumasulira zochita za Mulungu.

ANENERI

Mulungu amatuma mneneri wina aliyense ndi cholinga choti akwaniritse chikonzero chake

- Aneneneri amafotoko zochita za Mulungu kwa munthu.
- Ngati a nthenga a Mulungu, aneneri amalankhula choonadi cha Mulungu. Iwo amapereka uthenga wachiyembekezo ndi olimbikitsa anthu.
- Ngati aneneri amalosera zamtsogolo kudzera mwa Mzimu Woyera zimene Mulungu anakhazikitsa kuti akwaniritse
- Maulosi a m’Baibulo ndi oposa mphamvu kapena kuthekera kwa munthu. Amafotokoza zinthu mwachindunji ndi cholinga choti pasakhale kukaikanso ayi.

NJIRA ZOLOSERA

Pali njira ziwiri zimene Mulungu anagwiritsa ntchito pofuna kulankhula ndi aneneri.

MAU OLANKHURIDWA

Nthawi zambiri Mulungu amafotokozera mneneri mau amene iye amayenera kulankhula kwa anthu. Mwachitsanzo, Mulungu ananena ndi mneneri Yerememiya nati:

Yeremiya 1:7 Koma Yehova anati kwa ine, Usati, ndine mwana pakuti udzanka kwa yense amene ndidzakutumako iwe, nudzanena conse cimene ndidzakuuza. (Jeremiah 1:7)

Mu buku lonse la Yeremiya mau a Mulungu kwa Yeremiya anali oti:

Pita nupfuule n'makutu a Yerusalemu, kuti, Yehova atero, Ndikumbukira za iwe kukoma mtima kwa ubwana wako, cikondi ca matomedwe ako; muja unanditsata m'cipululu m'dziko losabzya lamo. (Yeremiya 2:2)

Yeremiya amangolankula mau amene Mulungu amamuuzza.

ULOSI WACHIONETSELO

Kuonjezera mau olankhulidwa, Mulungu amalamura aneneri kuti aonetsera uthenga wake. mwachitsanzo, Mulungu anauza Yereimiya kuti:

Yehova atero kwa ine: Udzipangire zomangira ndi magori, nuziike pakhosi pako; (Yereimiya 27:2)

Magoli amenewa amene Yereimiya anapanga amaonetsera goli la ukapolo limene lidzabwere pakati pa Israeli.

GWELO LA ULOSI

Gwero la ulosi wa Baibulo ndi Mulungu amene amavumbulutsa mau ake kwa munthu kudzera mwa Mzimu Woyera.

pakuti kale lonse cinenero sicinadza ndi cifuniro ca munthu; koma anthu a Mulungu, ogwidwa ndi Mzimu Woyera, analankhula. (2 Petro 1:21)

1 Akorinto 2:10 Koma kwa ife Mulungu anati onetsera izi mwa Mzimu; pakuti Mzimu asanthula zonse, zakuya za Mulungu zomwe. (I Corinthians 2:10)

Mulungu amalankhula mwachindunji zinthu zokhudza tsogolo

Ati Ambuye, amene azidziwitsa zinthu zonsezo ciyambire dzikolapansi. (Macitidwe 15:18)

Kumbukirani zinthu zoyamba zakale, kuti Ine ndine Mulungu, ndipo palibenso wina; Ine ndine Yehova, ndipo palibenso wina wofana ndi Ine; ndilalikira za cimariziro kuyambira paciyambi, ndi kuyambira nthawi zakale ndinena zinthu zimene zisanacidwe; ndi kunena, Uphungu wanga udzakhala, ndipo ndidzacita zofuna zanga zonse; (Yesaya 46:9-10)

Mulungu amadzutsa aneneri ake owona:

Yehova Mulungu wanu adzakuukitsirani mneneri wa pakati panu, wa abale anu, wonga ine; muzimvera iye; (Deuteronomo 18:15)

Mulungu amavumbulutsa chikonzero chake chamtsogolo kwa aneneri amenewa:

Amosi 3:7 Pakuti Ambuye Yehova sadzacita kanthu osaulula cinsinsi cace kwa atumiki ace aneneri. (Amos 3:7)

ANENERI ONYENGA

Naye Satana amatengera uneneri weniweni kudzera mwa asing'anga, amaula ndi anthu ena amatsenga. Koma njira zimenezi sizochokera kwa Mulungu. Mneneri Danieli anati:

Nayankha Danieli pamaso pa mfumu, nati, Cinsinsi inacitira liuma mfumu, angakhale anzeru, openduza, alembi, kapena alauli, sakhoza kuciululira mfumu; koma kuli Mulungu Kumwamba wakubvumbulutsa zinsinsi; Iye ndiye wadziwitsa mfumu Nebukadinezara cimene cidzagitika masiku otsiriza. Loto lanu, ndi masomphenya a m'mtima mwanu pakama panu, ndi awa: (Danieli 2:27-28)

Cholinga cha uneneri ndi kuwatengera anthu kwa Khristu Yesu.

Cifukwa cace ndikuuzani inu, kuti palibe munthu wakulankhula mwa Mzimu wa Mulungu, anena, Yesu ngwotembereredwa; ndipo palibe wina akhoza kunena, Yew ali Ambuye, koma mwa Mzimu Woyera. (1 Akorinto 12:3)

Baibulo limachenjeza zokhudza aneneri abodza (Mateyu 24:11,24; Marko 13:22). Munthu otchedwa mneneri wabodza adzaonekera masiku otsiriza (Chivumbulutso 13:11-17; 16:13; 19:20; 20:10). Baibulo limapereka njira zingapo zozindikira aneneri abodza:

- Amaphunzitsa anthu chiwerewere komanso chisawawa: II Petro 2:13.
- Amasocheretsa anthu kuti asamvere mau a Mulungu Deteronome 13:1-5.
- Amanena zinthu zabodza: Mateyu 24:23-23.
- Amanyenga anthu ndi zozizwa zabodza: Mateyu 24:11,24.
- Samaloseera mogwirizana ndi mau Mulungu (Aroma 12:6)
- Aneneri abodza samakhala ndi chipatso cha Mzimu Woyera pa moyo wao: Mateyu 7:15-16, Agalatiya 5:22-23.
- Zimeme amaloseera sizimachitika: Deteronome 18:20-22.

CHOLINGA CHA UNENERI

Baibulo limafotokoza cholinga chimene Mulungu amagwiritsira ntchito ulosi pofuna kulankhula kwa anthu ake.

POFUNA KUCHITIRA UMBONI MAU A MULUNGU

Uloso umene wakwaniritsidwa umaonetsa kuti mau a Mulungu ndi owonadi. Pa Yesaya 41:21-23 Mulungu akuuza milungu ya mafuko a dziko lapansi kuti iwonetsera mphamvu zake polosera zinthu zamtsogolo. Iwo sakanakwanitsa kutero chifukwa anali milungu yabodza.

Onetsani mlandu wanu, ati Yehova; turutsani zifukwa zanu zolimba, ati Mfumu ya Yakobo. Aziturutse, atichulire ife, cimene cidzaoneka; chulani inu zinthu zakale, zinali zotani, kuti ife tiganizire pamenepo, ndi kudziwa mamariziro ao; kapena tionetseni ife zinthu zimene zirinkudza. Chulani zinthu zimene zirinkudza m'tsogolo, kuti ife tidziwe kuti inu ndinu milungu; inde, citani zabwino, kapena citani zoipa, kuti ife tiopsyedwe, ndi kuona pamodzi. (Yesaya 41:21-23)

KUTSIKIMIZIRA MAU A MULUNGU:

Uloso umachitira umboni wa uthenga wa Mulungu weniweni:

Yeremiya 28:9 Mneneri amene anenera za mtendere, pamene mau a mneneri adzacididwa, pamenepo mneneri adzadziwika, kuti Yehova anamtuma ndithu. (Jeremiah 28:9)

KUPEREKA UPHUNGU KWA OKHULUPILIRA

Okhulupirira amalandira uphungungu ndi malangizo kuchokera ku ulosi ndipo amayenera kusamaritsa zinthu zimenezi:

Pakuti iye wakusowa izi ali wakhungu, wa cimbuuzi, woiwala matsukidwe ace potaya zoipa zace zakale, (2 Petro 1:9)

KUFUNIKA KOPHUNZIRA ULOSI

Pali zifukwa zitatu zikuluzikulu zimene tikuyenera kuphunzira ulosi:

1. Malemba onse ndi owuziridwa ndi Mulungu ndipo ndi opinduritsa.

Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa ciphunzitso, citsutsano, cikonzero, cilangizo ca m'cilungamo: kuti munthu wa Mulungu akhale woyenera, wokonzeka kucita nchito iri yonse yabwino. (2 Timoteo 3:16-17)

2. Ulosi umathandiza kuti timvetse chikonzero cha Mulungu kale, lero lino komanso mtsogolo mmene.

Cifukwa cace lembera zimene unazona, ndi zimene ziripo, ndi zimene zidzaoneka m'tsogolomo; (Cibvumbulutso 1:19)

3. Kumvetsetsa chikonzero cha Mulungu chatsogolo zimathandiza kuti musanyengedwe ndi Satana:

Pomwepo munthu akanena kwa inu, Onani, Kristu ali kuno, kapena uko musambvomereze; cifukwa Akristu onama adzauka, ndi aneneri onama nadzaonetsa zizindikiro zazikuru ndi zozizwa: kotero kuti akanyenge, ngati nkotheka, osankhidwa omwe. Onani ndakuuziranitu pasadafike. Cifukwa cace akanena kwa inu, Onani, Iye ali m'cipululu; musamukeko. Onani, ali m'zipinda; musabvomereze. (Mateyu 24:23-)

Chikonzero cha Mulungu chavumbulutsidwa zinthu zisanachitike ndi cholinga choti tisanamizidwe ndi Satana.

4. Pali madalitso apadera kwa onse amene asanthula zolembedwa mu mabuku a ulosi.

Wodala iye amene awerenga, ndi iwo amene akumva mau a cineneroco, nasunga zolembedwa momwemo; pakuti nthawi yayandikira. (Cibvumbulutso 1: 3)

MAPHUNZIRO A ULOSI

Ulosi wa Baibuo ndi gawo limodzi la “nyama” ya mau a Mulungu amene tinatchula kale mbuyomu. “nyama” ya uneneri ndi yovuta kumvetsetsa kusiyana ndi “mkaka” wa mau a Mulungu umene umafotokozerana mfundo zodziwika bwino lomwe za chikhulupiriro cha chachikhristu.

Ngati muli munthu oti mwangobadwa kumene mwatsopano, mukuyenera kuwerenga kaye magawo ena a mau a Mulungu musanayambe kuwerenga mabuku a ulosi. Werengani kaye mabuku a Uthenga Wabwino, Machitidwe, Makalata a Chipangano Chatsopano. Werenganinso

mabuku a ndakatulo, Chilamuro ndi mabuku a mbiri mu Chipangano Chakale. Pamene mukuwerenga mabuku amenewa, gwiritsani ntchito zimene mukuwerengazo.

Pamene mwapeza chidziwitso pang'ono cha magawo ena a Baibulo, mukhoza kuwerenga mabuku a ulosi ndipo musadera nkhwana ngati simukumvetsa ma ulosi onse amene akupezeka mu Baibulo. Pakhala pali maganizo osiyanasiyana pakati pa akatswiri a Baibulo pa tanthauzo la ma ulosi ena opezeka mu Baibulo.

MABUKU A ULOSI

Kupatula kuti tili ndi mabuku a ulosi, koma pali ma ulosi omwazikana amene akupezekanso mu zigawo zosiyanasiyana za Baibulo.

Ulosi oyamba kulembedwa mu Baibulo ukupezeka mu Buku la Genesis

ndipo ndidzaika udani pakati pa iwe ndi mkaziyo, ndi pakati pa mbeu yako ndi mbeu yace; ndipo idzalalira mutu wako, ndipo iwe udzalalira citende cace. (Genesis 3:15)

Ma vesi amenewa akuloseza zakubwera kwa Yesu Khristu amene kudzera mu imfa yake yofera machimo a anthu adzaononga Satana amene ali mdani.

Ndi zovuta kutchula ulosi wina ulionse umene walembedwa mu Baibulo. Koma inuyo mukuyenera kudziwa kuti pali ma ulosi ambiri amene akupezeka mu Baibulo lonse. Sikuti ulosi ukungopezeka mu mabuku amene ametchedwa kuti ndi a ulosi okha. Kudzera mukusanthula kwa Baibulo kwa nthawi yaitali, mutha kukwanitsa kuzindikira mitu ikuluikulu ya Ulosi imene imapezeka mu baibulo.

KUMVETSETSA ULOSI

Anthu ambiri amakhumudwitsidwa pamene akufuna kusanthula mabuku a ulosi m'baibulo. Chifukwa chakuti ulosi ndi ovuta kumvetsa kusiyana ndi mabuku ena, anthu ena amaona ngati kumvetsa ulosi wa baibulo sichinthu chimene wina aliyense akhoza kukwanitsa. Koma ndi zothekeka ndithu kuti timvetse ulosi wa Baibulo. Mulungu anafunitsitsa kuti Danili amvetse ulosi kotero kuti Iye anatumiza mngero kuti amufotokozere. Ndipo mngero anati:

Ndipo anandilangiza ine, ndi kulankhula nane, nati, Danieli iwe, ndaturuka tsopano ine kukuzindikiritsa mwaluntha. (Danieli 9:22)

Yesu anatenga nthawi yake pofotokozera ophunzira ake za ulosi wa Chipangano Chakale:

Cifukwa cace 5 khalani inunso okonzekeratu; cifukwa munthawi m'mene simuganizira, Mwana wa munthu adzadza. (Mateyu 24:44)

Pamene ophunzira a Yesu anafunsa zokhudza chimariziro cha nthawi, Yesu anafotokozera zizindikira za ulosi zimene ayenera kuyang'anira. Iye amafuna kuti iwo amvetse zinthu zimene zidzachitike mtsogolo. Yesu anati:

comweconso inu, pamene mudzaona zimenezo, zindikirani kuti Iye ali pafupi, inde pakhomo. (Mateyu 24:33)

Malingana ndi chiyambi cha buku la Chivumbulutso, ndi zoonekeratu kuti Mulungu amafuna kuti anthu ake azindikire kapena kumvetsa ulosi. Izi zili chomwechi ngakhale kuti anthu ena amanena kuti buku limeneli ndi lovuta kumvetsa.

CIBVUMBULUTSO ca Yesu Kristu, cimene Mulungu anambvumbulutsira acionetsere akapolo ace, ndico ca izi ziyenera kucitika posacedwa: ndipo potuma mwa mngelo wace anazindikiritsa izi kwa kapolo wace Yohane; (Cibvumbulutso 1:1)

ZIFUNGULO ZOTHANDIZA KUMVETSA ULOSI

Pali zinthu zingapo zothandiza kumvetsa ndi kumasulira ulosi wa Baibulo ndipo zina mwa mfundo zimenezi ndi izi:

1: MUTU WAUKULU WA ULOSI

Ambuye wathu Yesu Khristu ndiye mutu waukulu wa ulosi wa Baibulo. Koma pali mitu yambiri yokhudza ulosi wa Baibulo. Mwachitsanzo, pali maulosi okhudza chiweruzo cha Mulungu pa maiko oipa. Koma mutu waukulu wa ulosi wa Baibulo ndi cholinga cha Mulungu kudzera mwa Yesu Khristu.

Anatizindikiritsa ife cinsinsi ca cifuniro cace, monga kunamkomera ndi monga anatsimikiza mtima kale mwa iye, kuti pa tnakonzedwe a makwaniridwe a nyengozo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Kristu, za kumwamba, ndi za padziko. (Aefeso 1:9-10)

Ma ulosi onse a Baibulo ngakhakhale kuti akamafotokoza za chiweruzo cha Mulungu pa mafuko a dziko lapansi ndi zina zonse, izi zimakhala kuti zikugwirizana ndi chikonzero chonse cha Mulungu. Chikonzero chimenechi ndikubweretsa anthu onse kuti akhale ndi ubale oyenera ndi Mulungu kudzera mwa Yesu Khristu. Cholinga ndi kubweretsa zonse pansa pa Yesu Khristu.

Baibulo limafotokoza kuti mutu waukulu wa ulosi wa Baibulo ndi Yesu:

Ndipo ndinagwa pa mapazi ace kumlambira iye. Ndipo ananena ndi ine, Tapenya, usatero; ine ndine kapolo mnzako, ndi mnzao wa abale ako akukhala nao umboni wa Yesu; lambira Mulungu: pakuti umboni wa Yesu ndiwo Mzimu wa cinenero. (Cibvumbulutso 19:10)

Pamene mukusanthula ulosi wa Baibulo, muganizire za fuso ili. Kodi ulosi umeneu ukugwirizana bwanji ndi Yesu khristu amene ali mzimu wa ulosi. komanso funsani kuti kodi chikonzero chonse cha Mulungu pa ulosi umenewo ukugwirizana bwanji ndi Yesu.

2: BAIBULO LIMADZIMASULIRA LOKHA

Chifunguro kapena nsanamira yomasulira Baibulo ndi kuzindikira kuti Baibulo limamasulira ma ulosi ake omwe. Chitsanzo chabwino cha mmene Baibulo limadzimasulira ma ulosi ake omwe chikupezela pa Danieli 2. Apa mfumu yotchedwa nabukadineza inapatsidwa loto lochokera kwa Mulungu. Koma pamene mfumu imadzuka, simakumbukiranso za loto limeneli kotere kuti inasonkhanitsa amatsenga kuti anthandize kukumbukira ndi kusamasulira. Koma amatsenga nawo analephera. Mulungu anagwiritsa ntchito Danieli kuti akumbukire ndi kumasulira loto limeneli. Kufotokozera kwa maloto amenewa kukupezeka pa vesi 31 ndi 35. Ndipo kumasulira kwa malotowa kwaperekedwa pa Danieli 31-45. Ichi ndi chitsanzo cha mmene nthawi zambiri Baibulo limadzimasulira lokha.

Chipangano Chatsopano chimamasulira ma ulosi ambiri a Chipangano Chakale. Izi zili chomwechi chifukwa chakuti magawo ambiri a chipangano Chatsopano ndi kukwaniritsidwa kwa Chipangano Chakale. Mwachitsanzo, fanizirani ulosi uwu wa chipangano Chakale ndi kukwaniritsidwa kwake mu Chipangano Chatsopano.

. Ndipo ndidzadzibzalira iye m'nthaka, ndipo ndidzazitira cifundo Wosacitidwa-cifundo; ndipo ndidzati kwa Si-anthu-anga, Muli anthu anga; ndipo iwo adzati, Ndinu Mulungu wathu. (Hoseya 2:23)

ndi ife amenenso iye anatiitana, si a mwa Ayuda okha okha, komanso a mwa anthu amitundu? (Aroma 9:24

Ma ulosi okwaniritsidwa a Chipangano Chatsopano amaonetsera kukwaniritsidwa kwa ma ulosi okhudza kubwera kwa mesiya Yesu.

3: ULOSI OKAMBA ZA LERO KOMA OKWANIRITSIDWA MTSOGOLO

Mfundo imeneyi yomasulira ulosi imafotokoza kuti ulosi umene umafotokoza zakukwaniritsidwa kwake nthawi yomweyo ndi njira yoonetsera choonadi chachikulu kapena chinthu chimene chidzakwaniritsidwe mtsogolo.

Nthawi zambiri mu Baibulo, ulosi umakwaniritsidwa nthawi yomweyo imene wangoperekedwa, koma ulosi omwewonso umadzakwaniritsidwa mtsogolo kupatula kukwaniritsidwa kwake mu nthawi imene ulosiwo unaperekedwa.

Chitsanzo chabwino chikupezeka pa Ezekieli 28: 1-19 pamene akufotokoza za mfumu yaku Taya. Iyi inali mfumu yoipa imene zochitika zake ndi zofanana ndi olimbana ndi Khristu amene adzadzuka kumapeto kwa dziko. Pamene Mulungu anapereka ulosi umenewu kwa Ezekieli, zinakwaniritsidwa mmoyo wa mfumu imeneyi komanso ulosi umeneu udzakwaniritsidwa kumapeto a nthawi yoipa imene olamulira otsutsana ndi Khristu adzadzuka.

Pamene mukuwerenga ulosi ndi zofunika kufunsa mafunso awa:

1. Kodi ulosi umeneu umatanthauza chiani kwa anthu amene analandira ulosi nthawi imeneyi.
2. Kodi ulosi umeneu umakhudzanso zinthu zamtsogolo.

Kufunsa mafuso amenewa kukuthandizani kuti mukwanitse kumasulira ulosi moyenera komanso kupeza tanthauzo lake lenileni.

4: KUONA ZINTHU MWA UNENERI

Aneneri amafotokozera zinthu ngati kuti zinthuzo zichitika molumikizana ndi zinthu zimene zikuchitika nthawi yawo kapena kuti zichitika posachedwa. Mwachitsanzo, Yesaya analosera:

Mzimu wa Ambuye Yehova uli pa ine; pakuti Yehova wandidzoza ine ndilalikire mau abwino kwa ofatsa; Iye wanditumiza ndikamange osweka mtima, ndikalalikire kwa am'nsinga mamasulidwe, ndi kwa omangidwakitsegulidwa kwa m'ndende;

ndikalalikire caka cokomera Yehova, ndi tsiku lakubwezera la Mulungu wathu; ndikatonthoze mtima wa onse amene akulira maliro; ndikakonzere iwo amene alira maliro m'Ziyoni, ndi kuwapatsa cobvala kokometsa m'malo mwa phulusa, mafuta akukondwa m'malo mwa maliro, cobvala ca matamando m'malo mwa mzimu wopsinjika; kuti iwo achedwe mitengo ya cilungamo yakuioka Yehova, kuti Iye alemekezedwe. (Yesaya 61:1-3)

Pamene Yesu anawerenga ndime yochedwa ku Yesaya Pa Luka 4:17- 20 iye anasiyira pa mau akuti kulengeza chaka chokhazikika cha ambuye. Iye anatseka malemba ndikunena kuti malemba akwaniritsidwa mwa iye pa tsiku limenero. Ponena zimenezi, iye amanthauza kuti iye ndiye kukwaniritsidwa kwa mau amenewa. Iye ndi amene Mzimu wa Mulungu anali pa iye kuti akalarike uthenga Wabwino, kumasura ansinga ndi kulengeza ufulu kwa onse andende.

Koma zinali zofunika kuti Yesu anamariza kuwerenga ndi ndi mau oti “kukalarika Chaka cha Mulungu chokhazikika.” Iye sanawerenga ndime imene imakamba za tsiku lakubwezera la Mulungu wathu chifukwa chakuti nthawi inali isanafike. Padutsa zaka zokwana 2000 Yesu chilankhulire mau amenewa koma tsiku lobwezera la Mulungu silinafikebe.

Pamene alosi ukuperekedwa zimakhala ngati kuti zinthuzo zichitika nthawi yomweyo. kudzera muvumbulutso la Mzimu woyera, Yesaya anaona chikonzero chonse cha Mulungu. Iye amaona Yesu akulalikira, kumasura ansinga, andende ndi kubweretsa tsiku la chiweruzo cha Mulungu.

Yesaya amaona zinthu zimenezi ngati mmene munthu amaonera phiri limene liri patali. Zigwa zimene zili pakati pa mapiri sizimaoneka kufikira mutakwera pamwamba paphiri. Maonedwe a zinthu a uneneri amavumbulutsa chikonzero chonse cha Mulungu. Nthawi zina ulosi umafotokozeredwa ngati zinthu zimene zichitika posachedwa. Koma pamene maulosiwa akukwaniritsidwa pamakhala kuti padutsa nthawi yaitali ngati mmene ikuonetsera ndime ya buku la Yesaya. Pakadali pano Yesu sanakwaniritsebe malemba a tsiku la kubwezera kwa ambuye.

5: ULOSI OTENGERA MACHITIDWE A MUNTHU

Nthawi zambira ulosi wa Baibulo umatengera mmene munthu angachitire. Izi zikutanthauza kuti Mulungu amapanga zinthu zinazake malingana ndi mmene munthu atachitire. Ngati munthu

samvera mau a Mulungu, zinthu zinazake zimachitika. Ndipo chimodzimodzinso ngati munthu amvera mau a Mulungu ndiye kuti Mulungu amachita mosiyana ndi mmene amayera kuchitira.

Mulungu anati:

Koma mumvetu mau awa amene ndinena m'makutu anu, ndi m'makutu a anthu onse: Aneneri amene analipo kale ndisanakhale ine, nimusanakhale inu, ananenera maiko ambiri, ndi maufumu akuru, za nkhondo, ndi za coipa, ndi za caola. Mneneri amene anenera za mtendere, pamene mau a mneneri adzacididwa, pamenepo mneneri adzadziwika, kuti Yehova anamtuma ndithu. Pamenepo Hananiya anacotsa gori pa khosi la Yereimiya, nalityola. (Yereimiya 28:7-10)

Ma ulosi ambiri ndi ofuna kuti mupitirizebe kuwasanthula ndi cholinga choti muzindikire mmene munthu angachitire chifukwa kukwaniritsidwa kwa maulosi amenewa kukutengera kumvera kwa munthu. Chitsanzo chabwino ndi mfundo imene ikupezeka mu buku la Yona. Yona anuza anthu kuti Mulungu awononga mzinda wa Nenevi ngati anthu salapa pakadutsa masiku atatu. koma chiwonongeko sichinabwere chifukwa chakuti anthu aku Nenevi anamvera mau a Mulungu pakulapa machimo awo.

ULOSI WA CHIPANGANO CHAKALE

Ulosi wachipangano Chakale umakhazikika pa:

1.

Anthu a Israeli amene anali fuko limene Mulungu anadzutsa ndi cholinga choti adzionetsere yekha ku dziko lapansi. Mu nthawi imene Israeli anali ogawikana pawiri, ulosi umeneu umapita kwa Yuda ndi Israeli. Chitsanzo cha ulosi opita kwa Israeli ndi buku la Hoseya pamene Yoweri ndi ulosi umene umapita kwa Yuda.

2. Ma ulosi opita ku mafuko amene anazungulira Israeli. Mwachitsanzo pali ma ulosi amene akupita ku Babulo, Igupto, Edomu ndi maiko ena. Mwachitsanzo, Obadiya anapereka ulosi opita ku dziko la Edomu.

3. Ma ulosi okhudza zakubwera kwa Mesiya amene ndi Yesu Khristu. Maulosi amenewa angomwazika mu Chipangano chonse chakale sikuti ali mu buku limodzi la ulosi. Chitsanzo chabwino ndi Yesaya 7:14.

4. Ma ulosi okhudza dziko lonse lapansi, tsogolo lake, zinthu zimene zidzachitike mtsogolo komanso chimaliziro cha zinthu zonse. Buku la Danieli ndi chitsanzo chabwino cha ulosi umeneu. Chithunzi chili pansichi chikufotokozera mwachidule ma ulosi onse amene akupezeka mu chipangano Chakale. Ngakhale kuti ma ulosi amenewa amapita ku mafuko ena ake a nthawi imeneyo ndipo kuti anakwaniritsidwa nthawi yomweyo, koma ambiri mwa ma ulosi amenewa akufotokozera za zinthu zimene zidzachitike mtsogolo.

| Aneneri a Chipangono Chakale | | |
|------------------------------|--|---|
| Mneneri | Uthenga Wake | Nthawi ya uneneri |
| Yona | Chikondi cha Mulungu pa amitundu | Kwa Asuru ukapolo waku Babulo usanafike (800-650 B.B) |
| Nahumu | Chionongeko cha Nenevi chifukwa cha nkhanza zake | |
| Obadiya | Chionongemko ku Edomu chifukwa cha chinyengo chake | Ku Edomu asanapite ku ukapolo (800 BC) |
| Hoseya Amosi | Chikondi cha Mulungu pa Israeli wachigololo Kupya kwa chilango cha Mulungu pa anthu ake | Kwa Israeli asanapite ku Ukapolo (750 BC) |
| Yesaya Yeremiya Maliro | Kubwera kwa Mesiya Chiweruz kenako ulemelero utsatira | |

| | | |
|-----------|--|---|
| Yoweri | Chiweruzo chidzabwera ngati muliri | Yuda asanatengedwe kupita ku Ukapolo (800-606 BC) |
| Mika | Anthu a Mulungu ali pa mlandu | |
| Habakuku | Olungama adzakhala ndi moyo ndi chikhulupiro | |
| Zefaniya | Tsiku la Mulungu likubwera | |
| Ezekiyeli | Mulungu sanathane ndi Israeli | Ku Yuda nthawi ya ukapolo (606-606 B.C) |
| Danieli | Dzanja la Mulungu pa Israeli | |
| Hagai | Kuopsya kosadzipereka | Ku Yuda Utatha Ukapolo(536-400B.C) |
| Zakariya | Ulemelero wa Mesiya | |
| Malaki | Kuopsya koumitsa mtima | |

ULOSI WA CHIPANGANO CHATSOPANO

Pali maulosi ambiri amene amwazikana mu Chipangano Chatsopano ndipo ambiri mwa maulosi amenewa amafotokoza zinthu zimene zidzachitike pamene dziko lidzatsale pang'ono kutha. Mwachitsanzo, timawerenga ulosi opezeka pa Mateyu chaputala 24.

Pali buku limodzi mu Chipangano Chatsopano limene ndi la ulosi. Buku limeneli ndi buku la Chivumbulutso. Yohane amene anali ophunzira wa Yesu Khristu analandira vumbulutso kudzera mwa Mzimu Woyera. Buku limeneli ndi Vumbulutso la Yesu Khristu Yesu.

CIBVUMBULUTSO ca Yesu Kristu, cimene Mulungu anambvumbulutsira acionetsere akapolo ace, ndico ca izi ziyenera kucitika posacedwa: ndipo potuma mwa mngelo wace anazindikiritsa izi kwa kapolo wace Yohane; (Cibvumbulutso 1:1)

Yohane anauzidwa kuti:

Ine Yohane, mbale wanu ndi woyanjana nanu m'cisautso ndi ufumu ndi cipiriro zokhala m'Yesu, ndinakhala pa cisumbu cochedwa Patmo, cifukwa ca mao a Mulungu ndi umboni wa Yesu. (Cibvumbulutso 1:9)

Buku la Danieli liyenera kuwerengedwa limodzi ndi Buku la Chivumbutso chifukwa chakuti mabuku awiriwa ndi ofanana.

Pali kamasulidwe kosiyanasiyana ka ma ulosi a buku la Chivumbulutso. Nthawi zambiri kamasulidwe ka buku limeneli kamakhazikika pa nthawi imene zinthu zimene zofotokozeredwa mu bukuli zidzachitike. Koma chinthu chofunika kudziwa ndi chakuti zinthu zimene Baibulo limafotokoza zidzachitika. Mndandanda wa zinthu zikuluzikulu zimene zidzachitike ndi izi:

ZINTHU ZIKULUZIKULU ZAMTSOGOLO

- I. Baibulo limafotokoza kuti Yesu adzabwera pa dziko lapansi kudzatenga okhulupilira.
 - A. Mkwaturo: Pa I Atesalonika 4:13-18 amafotokoza zinthu zambira zokhudza zakubwera kwa Yesu. kubweranso kwa Yesu kumatchedwa mkwaturo: Vesi 16.
 1. Yesu mwini wake adzabweranso: Vesi 16.
 2. Padzakhala chiukitso cha anthu onse amene anafa ali okhulupilira vesi 16.

3. Okhulupirira onse adzakwaturidwa ndi kukakumana ndi Yesu mulengalenga Vesi 17.
4. Okhulupiriira onse amene anamwalira ndi amoyo adzayanjanitsidwa ndi Yesu Khristu: Vesi 17.

B. Chizuzo chachikulu

1. Chizuzo chidzachitika kwa miyezi yokwana makumi anayi ndi iwiri. Ndi masiku 1,260 Danieli 9:24-27.
2. Iyi idzakhala nthawi yowawitsa kwambiri. Pakhala nthawi zowawitsa zambiri koma nthawi imeneyi idzakhala yosiyana kwambiri ndi nthawi zonse.
 - a. Izi zidzachitika dziko lonse lapansi osati dera limodzi lokha. Chivumbulutso 3:10.
 - b. Anthu adzazindikira kuti chimariziro chafika: Chivumbulutso 6:6.
Kukula kwa chizuzo kudzakhala kwakukulu kumene sikunaonekepo: Mateyu 24:4-14.
3. Kufotokozeredwa kwa chizuzo: pali magawo angapo achiweruzo amene adzachitike pa dziko lapansi ndipo izi zikufotokozeredwa pa Chivumbulutso 6,8,9 ndi 16 komanso pa 24: 4-14.
4. Chifukwa cha chizunzo: kuipa kwa munthu kulangidwe, Satana agonjetsedwe, komanso kuti anthu onse akavomereze kuti Yesu ndi ambuye. Izi zizakwaniritsa chikonzero cha Mulungu pa dziko lonse lapansi chimene chinalankhulidwa pa Aefeso 1:8-9.

C. Nthawi ya nkhwaturo:

Anthu ena amakhulupilira kuti mkwaturo udzachitika chizunzo chisanafike kotere kuti anthu okhulupilira sadzakumana ndi chizuzo. Anthu ena amakhulupilira kuti mkwaturo udzachitika pakatikati pa chizuzo. Pamene ena amati mkwaturo udzachitika kumapeto kwa chizuzo. Koma ganizo lodziwika bwino lomwe ndi lakuti mkwaturo udzachitika chizuzo chisanafike. Maganizo osiyana amabwera chifukwa chakuti pali kumasulira kosiyana kwa ma ulosi amene alembedwa mu

buku la Danieli ndi Chivumbulutso. Koma chinthu chimene chili chofunika ndi kuzindikira kuti ndinu okhulupilira weniweni kotere kuti ndinu okonzeka kudzapita ndi Yesu.

- D. Ulamuliro wa Yesu wa dzaka 1000. Iyi ndi nthawi imene Yesu adzalamulire dziko lapansi ndi chilungamo chonse. (Zekariya 14:9 Danieli 7:14) Mzinda wa Yerusalemu lidzakhala likulu la boma. Nyengo imeneyi idzatha pamene Satana adzapandukira komaliza (Chivumbulutso 20:7-9) Koma Mulungu adzatumiza moto onse ndi kugonjetsa adani onse. Satana adzaponyedwa mu Nyanja ya moto kwa moyo wake onse.
- E. Chiweruzo: Anthu onse olengedwa adzaweruzidwa ndi Mulungu. Izi zimatchedwa kuti chiweruzo cha Muyaya. Anthu onse amene anamwalira ali osakhulupilira adzaukitsidwa ndi choling choti aweruzidwe. Chifukwa chakuti sanavomereze Yesu ngati mpulumutsi, adzalangidwa kwa muyaya ku Gahena. (Chivumbulutso 20:12-15). Koma anthu onse okhulupirira amene analapa machimo awo ndi kuvomereza kuti Yesu ndi ambuye adzakhala moyo wao onse ndi Yesu kumwamba kapena kuti pamaso pa Mulungu.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi yotsogolera osaonera.

2. Tchulani zolinga zitatu za ulosi wa Baibulo.

3. Tchulani mfundo zinayi zakufunika kophunzira ulosi

4. Tchulani mfundo zinayi zothandizira kumvetsa ulosi wa Baibulo

5. Kodi gwero la ulosi ndi chiani?

6. Fotokozerani tanthauzo la ulosi

7. Tchulani mitundu itatu ya kulankhula kwa ulosi mu Baibulo.

8. Kodi ndi njira ziti ziwiri zimene Mulungu anagwiritsa ntchito mu Baibulo popereka ulosi kwa anthu?

9. Kodi ulosi oyamba mu Baibuo ukupezeka pati?

10. Baibulo limafotokoza zinthu zothandiza kuzindikira uneneri wabodza. Ndipo tchulani zinthu zimenezi.

(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa buku ili)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Gwiritsani ntchito zimene mwaphunzira mu phunziro limeneli kuti musanthule mabuku awa.

CHIPANGANO CHAKALE.

___ Yesaya ___ Yereimiya ___ Maliro ___ Ezekiyeli ___ Danieli ___ Hoseya ___ Yoweli

___ Amosi ___ Obadiya ___ Yona ___ Mika ___ Nahumu ___ Habakuku ___ Zefaniya ___ Haggai

___ Zekariya ___ Malaki

Chipangano Chatsopano ___ Chivumbulutso.

2. Mulungu amalankhula mu Baibulo kudzera mu ulosi. Iye amagwiritsanso ntchito aneneri mu mpingo pofuna kulankhula kwa anthu ake.

Ndipotu Mulungu anailea ena m'Eklesia, poyamba arumwi, aciwiri aneneri, acitatu aphunzitsi, pamenepo zozizwa, pomwepo mphatso zamaciritso, mathandizo, maweruziro, malilime a mitundu mitundu. (1 Akorinto 12:28)

Uthenga umene aneneri alero amalandira si mbali imodzi ya mau a Mulungu olembedwa.

Uthenga umene amalandira umachitira umboni za Mau a Mulungu olembedwa. Zimene mneneri amanena zikuyenera kuweruzidwa ndi malingana ndi Baibulo.

Kuti mudziwe zambiri zokhudza ulosi, pezani Phunziro la Harvestime International lotchedwa “Utumiki wa Mzimu Woyera.” Phunziro limeneki limafotokoza mwatsatanetsate za mphatso za Mzimu Woyera.

CHAPUTALA 19

NJIRA YA CHIFANIZIRO

ZOLINGA

Pamapeto pa phunziri ili mukuyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osaonera.
- Kufotokozero tanthuazo la njira ya chifaniziro.
- Kutchula ma gulu anayi amene zifaniziro za Baibulo zimagawidwa.
- Kusanthula Baibulo pogwiritsa ntchito chifaniziro.

VESI YOTSOGOLERA

mthunzi wa zokoma zirinkudza, osati cifaniziro ceni ceni ca zinthuzo, sicikhozatu, ndi nsembe zomwezi caka ndi caka, zimene azipereka kosalekeza, kuwayesera angwiro iwo akuyandikira. (Ahebri 10:1)

MAU AYAMBA

Chaputala ichi chikufotokozero njira yosanthula Baibulo pogwiritsa ntchito njira ya chifaniziro. Njira imeneyi ifotokozeredwa komanso chitsanzo chiperekedwa mu gawo la zoonjezera pophunzira.

TANTHAUZO LA NJIRA IMENEYI

Kuti timvetse mmene tingasanthulire Baibulo pogwiritsa ntchito njira ya chifaniziro. Choyamba tikuyenera kumvetse tanthauzo la mau oti chifaniziro. Pali mau ambiri mu Baibulo amene amafotokozero tanthauzo la chifaniziro. Vesi yotsogolera ya chaputala chimenechi ndi Ahebri 10:1) imene imakamba za chilamuro ngati chifaniziro cha zinthu zamtsogolo. Mau oti chifaniziro ndi chimodzimidzi ndi chithuzithuzi. Chithuzithunzi ndi chifaniziro cha chinthu chimene chimaonetseracho, ngakhale kuti sichimoneka bwinobwino komanso chimasiyana ndi chinthu chimene chikuonetsera.

Mau akuti fanizo ndi chimodzimidzi ndi mau oti chifaniziro malinga ndi ndi Baibulo:

Komatu imfa inacita ufumu kuyambira kwa Adamu kufikira kwa Mose, ngakhale pa iwonso amene sanacimwa monga macimwidwe ace a Adamu, ndiye fanizo la wakudzayo. (Aroma 5:14)

Malingana ndi Baibulo, Adamu ndi fanizo la munthu wakudzayo kapena kuti ndi fanizo la munthu amene adzabwereyo. Adamu anali fanizo la Khristu amene amayenera kudzabwera mtsogoro.

Kuperekedwa kwa nsembe mu Chipangano chakale kunali fanizo la nsembe yomaliza imene idzaperekedwe mu Chipangano Chatsopano imene ndi Yesu Khristu:

Mzimu Woyera wodziwitsa nako, kuti njira yolowa nayo ku malo opatulika siinaonetsedwe, pokhala cihema coyamba ciri ciriri; ndico ciphiphiritso ca ku nthawi yomweyi, m'mene mitulo ndi nsembenso zinaperekedwa zosakhoza, ponena za cikumbu mtima, kuyesa wangwiro wolambirayo. (Ahebri 9:8-9)

Ndipo iye akadakhala padziko, sakadakhala konse wansembe, popeza pali iwo akupereka mitulo monga mwa lamulo; amene atumikira chifaniziro ndi mthunzi wa zakumwambazo monga Mose acenjezedwa m'mene anafuna kupanga cihema: pakuti, Cenjera, ati, ucite zonse monga mwa citsanzoco caonetsedwa kwa iwe m'phiri. (Ahebri 8:4-5)

Mau onsewa kaya ndi chifaniziro kapena fanizo ndi amodzi. Chifaniziro ndi munthu kapena chinthu chinachake chimene mu Baibulo Mulungu amagwiritsa ntchito pofuna kuonetsera munthu wina wake, chinthu china kapena zinthu zimene zidzachitike mtsogolo.

KUFOTOKOZERA NJIRA IMENEYI

Pamene tikugwiritsa ntchito njira ya chifaniziro, timasanthula munthu, malo kapena chinthu. Kenako timawerenga chinthu chimene ndi chifanizirocho. Mu njira ina tikhoza kunena kuti fanizo kapena chifaniziro chili ngati ulosi, chifukwa ma fanizo ena anakwaniritsidwa pamene ena akudikira kuti akwaniritsidwe.

Ngakhale kuti chifaniziro ndi chofunika pachokha, koma kufunikira kumaonekera kwambiri mwa munthu kapena chinthu chimene chifanizo chimaonetseracho. Chifaniziro ndi chithuzi chimene chimaonetsera za choondai chauzimu. Mwachitsanzo, kulumidwa ndi njoka kwa ana a Israeli ndi zinthu zoti zinachitikadi mu mbiri ya Israeli mu Chipangano Chakale. Timauzidwa pa

Numeri 21:6-9 kuti njoka imaluma anthu ndipo ena amamwalira. Koma Mose anapanga njoka ya Mkuwa ndipo wina aliyense amene amayang'ana njoka imeneyi amachiritsidwa. Zinthu zimenezi ndi chifaniziro cha imfa ya Yesu Khristu.

Ndipo monga Mose anakweza njoka m'cipululu, coteru Mwana wa munthu ayenera kukwezedwa; kuti yense wakukhulupira akhale nao moyo wosatha mwa iye.

(Yohane 3:14-15)

choonadi cha Baibulo nthawi zambiri chimafotokozeredwa mu njira yoti mwana akhoza kumvetsa. Koma pali choonadi china chimene ndi chobisika chimene chimakhalanso malo obisika. Zinthu zimenezi zimafuna kusanthula mozama kuti zimvetsetsedwe. Chiphunzitsu cha Baibulo chamafanizo chimabisidwa ngati chuma kotere kuti mukuyenera kutenga nthawi kuti mupeze zozama za mau a Mulungu.

Zifaniziro zonse zili mu magawo anayi amene ndi awa:

1. Anthu
2. Malo
3. Zinthu zochitika (miyambo ndi zinthu zina)
4. Zinthu zakuthupi

Chifaniziro chimodzi chachikulu chopezeka mu chipangano Chakale chimapezeka mu nkhani ya Yosefe. Werengani nkhani Yosefe pa Genesis ndi 37-50. Yosefe ndi chifaniziro cha Yesu Khristu. Pali zinthu zambiri zimene zinachitika mu moyo wa Yosefe zimene ndi chifaniziro cha zinthu zimene zidzachitike mu moyo wa Yesu Khristu. Zinthu zimenezi zikupezeka pa **mndanda uli pansiu.**

Kusanthula Baibulo Pogwiritsa Ntchito Chifaniziro

| | | |
|---------------------------|---|-----------------------|
| Kusanthula moyo wa Yosefe | ngati chifanizo cha | Yesu |
| Ndime | zochitika | Ndime Yohane 10:11 |
| Genesis 37:2 | Anali m'busa | |
| Genesis 37:3 | Amakondedwa ndi atate ake | |
| Genesis 37:4 | Abale ake amadana naye | |
| Genesis 37:8 | Abale ake anakana ulamuliro wake | |
| Genesis 37:11 | Bambo ake amazindikira za tsogolo lake ngati mneneMalira amazindikira za Yesu | |
| Genesis 37:13 | Atate ake anamutuma kwa abale ake. | |
| Genesis 37:13 | Anali okonzeka kuchita chifuniro cha Atate ake | |
| Genesis 37:18 | Abale ake anakonza chiwembu chofuna kumupha ngati mmene anachitira Pilato ndi Yesu (Rubeni anafuna kupeza njira yoti ampulumutse. | |
| Genesis 37:23 | Analandidwa mwinjiro wake. | |
| Genesis 37:28 | anagulitsidwa | |
| Genesis 37:26-28 | Anagulitsidwa ndi Juda (Judasi mu Chiheleni) | |
| Genesis 39:2 | Anasanduka otumikira | |
| Genesis 39:7-23 | Anakana mayesero | |
| Genesis 39:13-20 | anachitiridwa umboni wabodza | |
| Genesis 39:20 | Anavutika ngakhale anali osalakwa. | |
| Genesis 40:1-3 | Anali ndi ochimwa awiri nthawi ya mazuzo ake | |
| Genesis 41:14 | Iye anatuluka mu mndende yamanda. | |
| Genesis 41:57 | anapulumutsa dziko lapansi ku imfa. | |
| Genesis 47:1-2 | Abale ake anapeza mwai okumana ndi mfumu chifukwa cha iye | |
| Genesis 41:50 | Anali ndi mkazi wamitundu | |
| Genesis 50:14-21 | Anawonetse mtima okhululuka. | |

Moyo wa Yosefe unali ofunika kwambiri mwa iye yekha. Koma chofunika kwambiri chinali chifanizo chamtsogolo chimene ndi moyo wa Yesu Khristu. Malizitsani mndandanda uli mwambau popeza ndime zimene zikufanana ndi moyo wa Yesu Khristu mu mabuku a Uthenga Wabwino. Pamwamba pa mndandanda imeneu palembedwa chitsanzo choti mutsate mmene mungamalizire ziganizo zimenezi. Pamene mwamaliza mayeso odziyesa nokha, gwiritsani ntchito gawo la zoonjezera pophunzira kuti musanthule Baibulo potsatira njira ya chifanizo.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera.

2. Fotokozani tanthauzo la njira yosanthula Baibulo pogwiritsa ntchito chifaniziro

3. Kodi ndi mau ena ati ofananana ndi mau oti chifaniziro?

4. Tchulani magawo anayi amane chifaniziro cha Baubulo chimagawidwa.

5. Kodi ndi munthu wina uti mu Chipangano Chakale amene wagwiritsidwa ntchito ngati chifaniziro?

6. Kodi munthu ameneyu anali chifaniziro cha anthu.

(mayankho amafunso amenewa ali kumapeto kwa buku limeneli)

ZOONJEZERA POHUNZIRA

Zitsanzo zingapo za mafanizo zaperekedwa mu gawo limeneli ndipo mukhoza kugwiritsa ntchito kuti musanthule Baibulo pogwiritsa ntchito njira ya Chifaniziro

1. Werengani Isaki ngati chifaniziro cha Khristu (Genesis 21-28)

Zinthu zina zimene mukuyenera kuyang'anira. Isaki anali mwana okondeka yakhayo wa Abrahamu amene anali okonzeka kuperekedwa ngati nsembe. Iye mkazi wake anali Rabeka.

2. Santhulani moyo wa Rabeka ngati chifaniziro cha mpingo umene ndi mkwatibwi wa Khristu.

Rabeka amayenera kupanga chisankho chosiya banja lake ndipo iye amayenera kusiya chinachilichonse chakwawa.

3. Santhulani Nowa ngati chifaniziro cha chipulumutso (Genesis 6-8)

Dziwani kuti chilango cha tchimo ndi imfa ndipo kuti chigumura cha Nowa chinali chifaniziro cha chiweruzo cha Mulungu. Chitetetezo cha mu ngalawa chinakonzedwa mosamala. Mwachitsanzo munali chitseko chimodzi chabe komanso munali malo okwanira a muthu wina aliyense. Ngalawa imeneyi inamatidwa ndi cholinga choti madzi asalowe. Kodi izi zimaimilira bwanji chipulumutso cha Khristu Yesu.

4. Werengani kuyendayenda kwa ana a Israeli mu chipululu kumene kukupezeka mu buku la Eksodo, Numeri ndi Deteronome.

I Akorinto 10:11 amafotokoza kuti “zinthu zonsezi zinachitika ngati chitsanzo ndipo zinalembedwa ngati chidzudzuro kwa ife. Kuchoka ku Igupto ndi chifaniziro chosiya tchimo. Pamene kuyenda mu chipululu ndi chifaniziro cha moyo wa wakuthupi kapena kuti wachisawawa. Santhulani kulephera kwa Israeli mu chipululu. I Akorinto 10 amafotokoza kuti kulephera kwao kuli ndi kufunika.

5. Gwiritsani ntchito mndandanda uli pansiu kuti mupeze zifaniziro zina za m'baibulo. Mndandanda umeneu ndi ndi ochepa chabe chifukwa pali zifaniziro zambiri za Baibulo.

Mdandanda wa chifaniziro

Munthu

Aroni/wansembe

Yesu wansembe wamkulu

Abrahamu

Mulungu Tate

Davide

Khristu Mfumu

Esau

Munthu wakuthupi

Isaki

Khristu Mwana wa Mulungu omvera.

Yakobo

Esau Munthu wauzimu osiyana ndi Esau

Yona

chifaniziro cha imfa, kuikidwa mmanda ndi chiukitso.

Yosefe

Yesu

Yoswa

Yesu ngati mtsogoleri

Mekizedeki

Yesu ngati wansembe ndi mfumu

Mose

Yesu ngai momboli ngai olamula

Rebeka

Yesu mkwati wa mpingo

M'busa

Yesu m'busa wabwino

MALO:

Chipululu

Mayesero

Chipululu

Moyo wa munthu wakuthupi

Igupto

Tchimo

Kanani

Moyo odzadzazidwa ndi mzimu

Gomora/Sodomu

Wickedness Kuipa

Yerusalemu

kumwamba

Mzinda wa mpumuro

Yesu mtetezi wathu.

Refedimu

Moyo wauzimu

Zinthu zochika:

Nyanja yofira Kusiyanana ndi dziko

Zunthu zochitika mu mbiri

Imfa, Kuikidwa mmanda, chiukitso cha Yesu

Nkhondo Nkhondo yauzimu

Kuyeretsa Kuyeretsa

Zochitika zachilengedwe:

Moto Kupezeka kwa Mulungu kapena chiweruzo

Madzi osefukira Chiweruzo

Mvula Madalitso

Madzi ungwiro

Mphepo Ukulu ndi mphamvu

Miyambo yochitika

Zopereka za Israeli

- Zopereka za nsembe yauchimo: Levitiko 4:1-6. Chifaniziro Cha Chipulumutso cha Yesu kudzera mwazi umene Yesu anapereka.
- Zopereka zopsereza: Munthu amene amapereka nsembe imeneyi amakhala kuti akuzindikira kuti kudzipatura ndi koyenera kuti munthu akhale ndi chiyanjano ndi Mulungu. Levitiko 1:1-4
- Chopereka cha mtendere. Izi zimagotokozera mfundo yokhala pa chiyanjano ndi mtendera ndi Mulungu. Gawo limodzi la chopereka chimechi limaotchedwa pa guwa la Mulungu.

Madyelero a Israeli

Pasaka: nkhesa inali chifaniziro cha Yesu ndi mwazi wa chipulumutso: Ekisodo 12:3-5; 11-

Pentekotse: Tanthauzo la chikondwewero cha Pentekoste linakwaniritsidwa pa tsiku la Pentekoste pamene Mzimu Woyera anabwera pa ophunzira pa chipinda chapamwamba: Levitiko 23:15-17 and Machitidwe 4.

Madyelero a misasa: izi sizinakwaniritsidwebe. Chifaniziro chimenechi chikuonetsera chikondwewero chachikulu pamene anthu onse opulumutsidwa adzasonkhanitsidwa pamodzi pa mpando wa chifumu wa Mulungu. Deteronome 16:13-15

ZINTHU ZAKUTHUPI

Likasa:

Mulungu anapereka likasa ngati malo amene Iye akhoza kukumana ndi anthu ake.

Kunja kwa chihema. Awa anali malo amene anthu amakumana ndi ansembe. Makatani amene amazungulira likasa la Mulungu amaimira kulekanitsidwa ndi tchimo. Koma chifukwa chakuti zotchingira zimene zinali za nsalu, izi zimangosonyeza kuti zinali zinthu zosakhalitsa. Chitseko cha mkati mwachihema chimamutengera munthu pamaso pa Mulungu.

Malo oyera. Amaimira utumiki wa unsembe. Mkati mwa malo amenewa munali zoikilamo nyali za golide zimene zinali chifanizo cha kuchitira umbono. Komanso munali guwa la golide limene limaimira kupembedzera ndi kulambira.

Malo oyeretsetsa. Awa anali malo apadera okhalamo a Mulungu. Nsalu kapena katani imene imalekanitsa malo amenewa ndi malo oyera ikusonyeka kuti kunali kovuta kuti munthu afikire Mulungu. Mpando wachifundo umaonetse kuti Mulungu amene ndi wachilungamo ndi wachifundo chifukwa chakuti anakheta mwazi. Kudzera mu likasa la Mulungu, Iye anawonetsa zimene adzachite mtsogolo. Iye adzapereka mwai kwa munthu kuti akhale pachiyanjano ndi Mulungu kudzera mwa Yesu Khristu. Iye adzakhala mu kachisi wauzimu amene ndi Mpingo. Komanso iye adzakhala mwa okhulupirira wina aliyense. Izi zikutanthauza kuti phunziro limene tikulipeza kuchokera ku likasa ndi lakuti likasa ndi chifanizo cha Yesu Khristu.

Zinthu zopezeka mu likasa

Brass: Chiweruzo

Golide Ulemelero

Siliva Chipulumutso

Mitundu ya Chifaniziro

Mtundu ofira mazuzo

Mtundu Woyera Chiyero

Chifaniziro za chakudya

Mkate moyo opitilira

Chipatso kuchulukana kapena kubala

Zinthu zolengedwa

Mbalame Mizimu yoipa

Nsomba Anthu

Mbuzi uchimo wa munthu ochimwa.

Nkhosa Yesu ndi Nsembe yake yagwiro

Njoka Satana

Nkhosa anthu a Mulungu

KUSANTHULA BAIBULO KUGWIRITSA NTCHITO CHIFANIZIRO

Kusanthula _____ ngati chifaniziro cha _____

Ndime zinthu zochitika ndime

NJIRA ZINA ZOSANTHULIRA BAIBULO

Njira za kusanthula Baibulo mwaluso zomwe zafotokozoredwa mu bukhu lino ndi zopindulitsa koposa m'moyo komanso utumiki wanu. Komabe pali njira zina za kasanthulidwe ka Baibulo zomwe anthu akhoza kugwiritsa ntchito zomwe zaperekedwa m'chigawo chino cha zoonjezera. Ngakhale kuti njirazi ndi zosangalatsa komanso zotha kuonjezera chidziwitso chanu, njirazi si zopindulitsa kweni kweni poyerekeza ndi zija zomwe taphunzira kale. Chotero m'chigawo chino tangopereka kafotokozedwe kochepe chabe ka njirazi:

NJIRA YA NDALE:

Njirayi imagwiritsidwa ntchito posanthula nkhani zokhuzana ndi ndale za maiko a m'Baibulo. Imathandizira kumvetsa bwino momwe maiko a mu nthawi ya Baibulo amayendetsedwera. Kuti muchite mtundu uwu wa kasanthulidwe ka mau mukuyenera kupeza:

1. Kupeza mtundu wa ulamuliro: wa nkhaza kapena wotsata malamulo
2. Nzeru ya ulamuliro: demokalase kapena nzeru zina.
3. Dera la ulamuliro:
 - a. Dera lolamulidwa
 - b. Magawo a deralo
 - c. Maudindo a ulamulirowo
 - d. Mphamvu ya dera pa ulamuliro
4. Atsogoleri a ulamuliro
5. Machitachita a ulamuliro
 - a. Kayendetsedwe
 - b. Zachuma
 - c. Nkhondo ndi ubale ndi maiko ena
 - d. Nkhani za malamulo
6. Mphamvu ya magulu a zipembedzo pa ulamuliro wa boma
7. Mphamvu ya ulamuliro wa boma nkhani yomwe mukusanthulayo

NJIRA YA MAKHALIDWE

Njira iyi imaona za chikhalidwe, machitidwe ndi maganizidwe a anthu a m'Baibulo. Imafuna kufufuza zifukwa zomwe anthu a m'Baibulo amachitira zomwe anachitazo. Zitsanzo za zomwe njira ya Kasanthulidwe ka Baibulo ka Nzeru imayang'ana ndi monga:

1. Kufufuza zolinga za utumiki wa Chikristu mu Afilipi 1:14-19.
2. Kusanthula mphamvu ya dera la Solomo pa ulamuliro wake.
3. Kusanthula zomwe Yesu anamva ngati munthu.
4. Kafukufuku wa zomwe Afarisi amachita kwa Yesu ndi zifukwa zake
5. Kafukufuku wa maganizo ndi machitidwe a Eliya potha pa mpikisano wa pa Phiri la Karimeli.
6. Kusanthula zolinga za anthu omwe amaletsa Nehemiya kumanganso linga la Yerusalemu.

NJIRA YA UKATSWIRI WA CHIDZIWITSO CHA ZINTHU ZAMOYO NDI ZOPANDA MOYO

Njira iyi imayan'ana kwambiri zinthu monga zomera, nyama, miyala ndi zolengedwa zina zosiyana-siyana. Kuti muchite msanthulo uwu, onani mutu womwe mukuphunzira ndi mavesi omwe akukamba zimenezo kenaka ndikuona kufunika kwake pa moyo wauzimu. Chitsanzo cha momwe kasanthulidwe aka kangaonjezere chidziwitso chanu pa Mau a Mulungu nachi:

Mutu: Mpiru (mbeu ndi chomera)

Mavesi: Mateyu 13:31; 17:20; Marko 4:31; Luka 13:19; 17:6

Phunziro lauzimu: Mbeu ya mpiru imatha kukula mwina ngati mikono itatu ndi theka. Mbeu iyi ikugwiritsidwa ntchito ndi Yesu pofuna kuyerekeza Ufumu wa Mulungu ndi chikhulupiriro. Mayambidwe opepuka a Ufumu wa Mulungu afotokozeredwa ndi fanizo la mbeu yaing'ono kwambiri. Ngakhale imayamba mochepa, kumapeto kwake imakula ndi kukhala mtengo waukuru. Umu ndi momwe Ufumu wa Mulungu umakhalira. Yesu ananenanso kuti ngati anthu angakhale ndi chikhulupiriro chaching'ono ngati kambeu ka mpiru atha kuchita zinthu zazikuru.

NJIRA YA MOYO WA TSIKU NDI TSIKU

Iyi ndi njira imene amafufuza za gulu la anthu, makhalidwe ndi maubale awo wina ndi mnzake m'gulumo. Mumayamba kusanthula mabanja, mudzi, boma ngakhale maunduna, za ntchito, mtundu wa anthu, chipembedzo, maphunziro, zotsangalatsa ndi za maluso. Chitsanzo chabwino chitha kukhala maubale a tsiku ndi tsiku. Werengani Aefeso 5:21-6:9 ndi Akolose 3:18-4:1. Chitsanzo china gawo la azimayi mu magawo osiyanasiyana a m'Baibulo.

NJIRA YA CHIKHALIDWE CHA ANTHU

Iyi ndi njira yomwe timasanthula munthu, chilankhulo, chikhalidwe, momwe amakulira, ndi mbiri yake. Mbiri ya anthu imafufuzidwa kudzera nkukumba zinthu zomwe anthu akale amagwiritsa ntchito. Mwachitsanzo cha kusanthula chilankhulo chitha kukhala kuyerekeza zilankhulo za pa Nsanja ya Babulo (Genesisi 11) mpatso ya malilime pa tsiku la Pentekosite (Machitidwe 4). Chitsanzo cha kusanthula chikhalidwe cha anthu a m'Baibulo chitha kukhala kuona chipembedzo, luso, nyimbo, ukatswiri ndi zolembalemba za anthu a nthawi ya Baibulo. Mutha kusanthula nyimbo za ana a Israel komanso zida zawo zoyimbira zomwe zatchulidwa m'Baibulo.

KUSUNGA ZOMWE MUKUPEZA POSANTHULA MAU

Nkofunika kusunga mosamala zomwe mukupeza pamene mukusanthula Mau a Mulungu. Mwina mudzafuna kusanthula mutu womwewo, bukhu kapena ndime yomweyo nthawi ina yake. Mwina mutha kufuna kugawana ndi ena zomwe mwakhala mukuphunzira nkusanthula kwanu.

Njira yabwino yosungira zomwe mukupeza ndi kusunga mafailo a ndemanga zanu. Mutha kusunga mafailo anu molingana ndi mabuku, mitu ya nkhani, kapena maina a anthu omwe mwasanthula. Magawo atatu akulu amenewa atha kuoneka motere:

1. Mabuku: Pangani gawo lomwe muzisungiramo za mabuku omwe mukusanthula, machaputala, ndime, mavesi, mau amodzi paokha. Onesetsani kuti mukuika mwadongosolo – kuyambira Genesisi mpaka Chibvumbulutso.
2. Mitu ya Nkhani: Pamene mukusanthula mitu yosiyana-siyana, sungani moyenera. Mwachitsanzo, ngati mukuphusanthula za pemphero, ikani pamene pali nkhani zokhuzana ndi pemphero. Kaya mafanizo a Yesu, kapena maina a Mulungu, chitani chimodzi-modzi.
3. Anthu: Gawo ili likhala ndi maina a anthu osiyana-siyana omwe mwasanthula monga Mose, Davide, Yosefe ndi ena ambiri. Asanjeni bwino lomwe molingana ndi maina awo.

MAYANKHO A MAFUNSO ODZIYESA NOKHA

CHAPUTALA 1:

1. Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa ciphunzitso, citsutsano, cikonzero, cilangizo ca m'cilungamo: kuti munthu wa Mulungu akhale woyenera, wokonzeka kucita nchito iri yonse yabwino. (2 Timoteyo 3:16-17)
2. Mau oti “Baibulo” amanthauza “mabuku.”
3. Mau oti “Malemba amanthauza “malemba oyera.”
4. Chipangano Chakale ndi Chipangano Chatsopano
5. Chilamulo, mbiri, ndakatulo, ndi uneneri.
6. Mabuku a Uthenga Wabwino, mbiri, makalata, uneneri.
7. Mau oti “chipangano” amanthauza “mgwirizano.”
8. Pa chiphunzitso, chidzudzulo, chilangizo, ndi chikonzero mchilungamo (2 Timoteyo 3:16-17).
9. Baibulo silimadzitsutsa lokha ndipo logwirizana mchiphunzitso chake.
10. Baibulo linalembedwa mosiyana-siyana.
11. a = T, b = T, c = F, d = F, e = F
12. Yesu. Luka 24:44-48

CHAPUTALA 2:

1. Kupfuula kwanga kuyandikire pamaso pano, Yehova; Mundizindikiritse monga mwa mau anu. (Masalimo 119:169)
2. 39
3. 27
4. Mukamawerenga Baibulo mwa apa ndi apo simungathe kulimvetsa bwino. Mukuyenera kuliwerenga mwa dongosolo kuti muthe kumvetsa zonse zolembedwamo.
5. – Kuwerenga tsiku ndi tsiku
 - Kuwerenga mosankha
 - Kuwerenga ndi pemphero
 - Kuwerenga mwa dongosolo

CHAPUTALA 3:

1. (Yohane 8:47) Iye wocokera kwa Mulungu amva zonena za Mulungu; inu simumva cifukwa cakuti simuli a kwa Mulungu,
2. Chifukwa chakuti amafuna kuliwerenga ngati bukhu wamba.
3. Chinthu chofunika kuchitika china chisanachitike
4. Kumdziwa Mulungu ndi kumubvomereza Yesu ngati Mpulumutsi
5. Okhulupirira omwe ayaitanidwa ngati aphunzitsi. Mzimu Woyera
6. Mzimu Woyera
7. Mkaka ndi choonadi cha Mau a Mulungu koma chosavuta kumvetsa.
8. Nyama ndi choonadi cha Mau a Mulungu koma chozama ndi chovuta kuchimvetsa.
9. - Kukhumba mkaka
 - Kukhala okhulupirika ku Mau a Mulungu
 - Kusakasaka nyama
10. Kuika nthawi ya padera tsiku ndi tsiku kuwerenga Mau

CHAPUTALA 4

- Buku koma adzapulumutsidwa mwa kubala mwana, ngati akhala m'cikhulupiro ndi cikondi ndi ciyeretso pamodzi ndi cidziletso. (1 Timoteyo 2:15)
- Zikutanthauza kuti mukuyenera kumvetsa chomwe chikukambidwa komanso yemwe akuuzidwa. Mukuyeneranso kutanthauzira moyenera ndi kugwiritsa ntchito zomwe mwaphunzirazo.
- Kuuziridwa kwa mau kwa Baibulo kumatanthauza kuti lemba lirilonse m'mabuku a zolembedwa zoyambirira za Baibulo linauziridwa ndi Mulungu.
- Kuuziridwa kwatunthu kwa mau kwa Baibulo kumatanthauza kuti gawo liri lonse la Baibulo linauziridwa ndi Mulungu, osati kagawo kochepe chabe ka Baibulo.
- Malamulo ake ali motere:
 - Lamulo la ulamuliro wa Mulungu: Timabvomereza kuti Baibulo liri ndi ulamuliro wonse popeza kuti linauziridwa ndi Mulungu.
 - Lamulo lotanthauzira zomwe zalembedwa: Baibulo limatanthauza zomwe lanena.
 - Lamulo loganizira zomwe zazungulira nkhaniyo: Vesi iliyonse ikuyenera kutanthauziridwa molingana ndi momwe mavesi oyandikana nawo aliri.

- Lamulo la kutchulidwa koyamba: Chinthu, chochitika, kapena mau akatchulidwa koyamba m’Baibulo, zimapereka mfungulo ya tanthauzo lake ngakhale m’ malo ena onse komwe angatchulidwe.
- Lamulo lobwereza: Pamene chinthu chabwerezedwa-bwerezedwa m’Baibulo ndiye kuti ndi chofunika kukhala nacho chidwi.
- Lamulo la bvumbulutso lokwaniridwa: Chiphunzitso cha choonadi cha Mau a Mulungu chisangochokera pa vesi limodzi lokha ayi. Zonse zimene Baibulo likukamba pa nkhani imeneyo zikuyenera kuonedwa.

CHAPUTALA 5

1. Kuyambira kale ndinadziwa mu mboni zanu, Kuti munazikhazika kosatha, (Masalimo 119:152)
2. k, l, c, d, e, g, f, j, h, i, b, a.
3. Pamene
4. Kasanthulidwe ka zinthu zopezeka m’ madera omwe anthu a m’Baibulo ankakhala. Ndi ukatswiri wodziwa momwe anthu ankakhalira pongopima zinthu zomwe ankagwiritsa ntchito.

CHAPUTALA 6

1. Mboni zanu ndizo zolungama kosatha; Mundizindikiritse izi, ndipo ndidzakhala ndi moyo. (Masalimo 119:144)
2. Mfundo yaikulu yoyamba isakhale pansu pa Mfundo I. Ikuyenera kukhala payokha moonetsedwa ndi malemba awa (II). Onani zomwe mwaphuzira pa kapangidwe ka mlozo.
3. Mulifupi ndi mulitali.
4. Kuika zizindikiro ndi njira imodzi yowonetsera mavesi omwe ndi ofunika kwambiri m’Baibulo.

CHAPUTALA 7

- c. Munditsegulire maso, kuti ndipenye Zodabwiza za m’cilamulo canu. (Masalimo 119:18)
- a. Onani zizindikiro zomwe zalembedwa mu chaputala 9.
- b. Onani zolinga zomwe zalembedwa mu chaputala 9.

- c. Amene amati akulalikira mau osati akulalikiradi Mau a Mulungu. Amenewa ndi aphunzitsi onyenga.
- d. Mulungu adzaonjezera miliri pa iwo monga momwe Chibvumbulutso 22:18-19 akunenera.
- e. Adzachotseredwako gawo lawo kuchokera m’bukhu loyera ndi mu mzinda woyera komanso zinthu zonse zolembedwa m’Mau a Mulungu. Chibvumbulutso 22:18-19.
- f. Mulungu
- g. Mau a Mulungu.
- h. Mkaka ndi nyama
- i. Mose

CHAPUTALA 8

1. Maso anga anakumika malonda a usiku, Kuti ndilingirire mau anu.
(Masalimo 119:148)
2. Njira iyi imatsindika kugwiritsa ntchito chidziwitso m’moyo ndi mu utumiki.
Imathandizira kuti munthu akhale wodzipereka kwatunthu kwa Mulungu.
3. Ndondomeko yake nayi:
 - Kulemba zandimeyo
 - Kupeza vesi lotsogolera
 - Kupeza mutu wa nkhani
 - Kulemba mwachidule
 - Kulingalira
 - Kugwiritsa ntchito
4. Kuwerenga kapena kumva Mau pakokha sikokwanira. Mukuyeneranso mugwiritse ntchito zomwe mwawerenga ndi kumvazo m’moyo ndi mu utumiki wanu (Yakobo 1:22-25).
5. Satana amalimbana ndi njira iyi popeza amada nkhwawa kuti anthu akamasanthula Mau a Mulungu ndi cholinga chakuti awagwiritse ntchito, moyo wawo sukhala chimodzimodzi ndipo iye sapeza mpata.

CHAPUTALA 9:

1. Mnyamata adzayeretsa mayendedwe ace bwanji? Akawasamalira monga mwa mau anu. (Masalimo 119:9)
2. 2, 1.
3. Pangani kafukufuku woyamba, pangani tchatu chanu, pangani mlozo wanu.
4. – Mutu wa bukhu
 - Nkhani yaikulu
 - Wolemba
 - Olemberedwa
 - Cholinga
 - Mfundo yaikulu m'moyo kapena mu utumiki

CHAPUTALA 10:

1. Ndinawabisa mau anu mumtima mwanga, Kuti ndisalakwire Inu. (Masalimo 119:11)
2. Kusanthula Mau kudzera m'machaputala
3. – Sankhani mutu wa chaputalacho
 - Ikani zizindikiro m'malire a ndime
 - Pangani tchatu cha chaputala
 - Pangani mlozo wa chaputala

CHAPUTALA 11:

1. Potsegulira mau anu paunikira; Kuzindikiritsa opusa. (Masalimo 119:130)
2. – Santhulani chaputala
 - Onani zomwe ziri mu ndimeyo mosamalitsa
 - Pangani tchatu cha kusanthula ndime
 - Pangani mlozo wa kusanthula ndime
3. 3, 2, 4, 1
4. 4, 5, 1, 2, 3
5. 3, 2, 4, 1

CHAPUTALA 12:

2. Lilime langa liyimbire mau anu; Pakuti malamulo anu onse ndiwo olungama. (Masalimo 119:172)

3. Zomwe zazungulira nkhaniyo
4. Santhulani vesilo molingana ndi zomwe zalembedwa mozungulira.
 - Onani mavesi a pafupi
 - Pangani tchatu cha vesi
 - Pangani mlozo wa vesi

CHAPUTALA 13:

1. Pakuti indetu ndinena kwa inu, Kufikira litapitirira thambo ndi dziko, kalemba kakang'ono kamodzi kapena kansonga kace kamodzi sikadzaeokera kucilamulo, kufikira zitacididwa zonse. (Mateyu 5:18)
2. – Sankhani mau
 - Santhulani mauwo mogwirizana ndi ndime yomwe akupezekamo
 - Pezani tanthauzo lake
 - Lembani mwachidule zomwe mwapeza posanthula mauwo
3. Mau akulu ndi mau omwe ndi ofunika kwambiri ku tanthauzo la vesi. Nthawi zina amakhala mau ovuta kuwamvetsa koma nthawi zina amakhala kuti abwerezedwa kwambiri.
4. Mau oti “kudziletsa” mau oti atha kukhala abwino kuwasanthula osati enawo.

CHAPUTALA 14:

1. Cifukwa cace ndikonda malamulo anu Koposa golidi, Inde golidi woyengeka, Cifukwa cace ndiyesa ngolunjika malangizo anu onse akunena zonse; Koma ndidana nazo njira zonse zonyenga. (Masalimo 119:127-128)
2. Njira yosanthula Baibulo pa Mutu. Cholinga cha njira imeneyi ndi kufuna kuzindikira zinthu zonse zimene Baibulo limaphunzitsa pa mutu umene mwasankha.
3. Sangani njira.
 - Sankhani ndime imene mukuna kusanthula.
 - Bweretsani zinthu zonse pamodzi.
 - Fotokozerani zinthu zimene mwapeza mwachidule.

CHAPUTALA 15

1. Koma izi zinacitika kwa iwowa monga zoticenjeza, ndipo zinalembedwa kuticenjeza ife, amene matsirizidwe a nthawi ya pansu pano adafika pa ife. (1 Akorinto 10:11)
2. Njira yosanthula Baibulo Poyang'anira moyo wa Munthu timaphunzira zambiri kuchokera pa zimene anthuwa anadutsamo.
 - Sankhani munthu amene mukufuna kusanthula.
 - Bwerezetsani zinthu zonse pamodzi.
 - Unikirani zinthu zimene mwapeza.
 - Gwiritsani ntchito zinthu zimene mwapeza.

CHAPUTALA 16.

1. 7, 8, 5, 3, 4, 2, 1, 6, 9, 10
2. Mboni zanu nzodabwiza; Cifukwa cace moyo wanga uzisunga, (Masalimo 119:129)
3. Kusanthula Baibulo poyang'anira chiphunzitso kumakhazikika posanthula zithu zonze zimene Baibulo limaphunzitsa.
4. – sankhani mutu umene mukufuna kusanthula
 - Fotokozerani tanthauzo la chiphunzitso chimene mwasankha.
 - Sankhani ndime imene mukufuna kusanthulaa.
 - Bweretsani pamodzi zinthu zonse zokhudza chiphunzitsa chanu.
5. Chiphunzitso ndi kubwera pamodzi ka maphunziro osiyanasiyana. Chiphunzitso chimakhala ndi zonse zimene Baibulo limaphunzitsa.

CHAPUTALA 17:

1. Ndikulemekezani kasanu ndi kawiri, tsiku limodzi, Cifukwa ca maweruzo anu alungama. (Salimo 119:164)
2. b,c, a.
3. c, a, b, d.
4. kofanana
5. motsutsana.
6. Kuimilira.

CHAPUTALA 18:

1. Ndipo anati kwa iwo, 5 Awa ndi mauwo ndinalankhula nanu, paja ndinakhala ndi inu, kuti ziyenera kukwanitsidwa zonse zolembedwa za Ine m'cilamulo ca 6 Mose, ndi aneneri, ndi masalmo. (Luka 24: 44)
2. Kuchitira umboni za Mau a Mulungu kuti owona
 - Kutsimikizira za Mau a Mulungu.
 - Kuphunzitsa okhulupilira.
3. Mau onse ndi opindulitsa kuwasanthula. Ulosi wa Mulungu umaonetsera zinthu za mtsogolo, zakale komoanso zimene zikuchitika mu nthawi ya loro mu chikonzero cha Mulungu. Kumvetsetsa chikonzero cha Mulungu zimathandiza kuti tisanyengedwe ndi chinyengo cha Satana. Komanso madalitso apadera akuperekedwa kwa anthu onse amene amawerenga Ulosi.
4. Kuzindikira Yesu Khristu ndi Mutu waukulu wa ulosi.
 - Kuzindikira kuti nthawi zambiri Baibulo limadzimasulira lokha.
 - Kumvetsetsa lamuro la kutchulidwa kachiwiri.
 - Kumvetse kaonedwe oyenera ka ulosi.
 - Kuzindikira kuti ulosi umatengera mmene munthu kapena anthu achitira zinthu zawo.
5. Mulungu.
6. Ulosi umatanthauza kulankhula pansu pakudzodzedwa ndi Mulungu.
7. Uthenga ochokera kwa Mulungu.
 - Ulosi wa zinthu zimene zidzachitikwe mtsogolo.
8. Ulosi olankhuridwa komanso wachiometsero.
9. Genesis 3:15. Umene ndi ulosi wa Mesiya.
10. Werengani njira zozindikira ulosi wachinyengo zimene zalembedwa pa chaputala 20.

CHAPUTALA 19:

1. mthunzi wa zokoma zirinkudza, osati cifaniziro ceni ceni ca zinthuzo, sicikhozatu, ndi nsembe zomwezi caka ndi caka, zimene azipereka kosalekeza, kuwayesera angwiro iwo akuyandikira. (Ahebri 10:1)
2. Njira yosanthula Baibulo pogwiritsa ntchito chifaniziro ndi njira imene imasanthula zinthu, malo kapena munthu amene ndi chifaniziro cha chinthu china. Chifaniziro chimaonetsero chikonzero cha Mulungu mtsogolo. Ngakhale kuti chifaniziro ndi

chofunika pachokha koma, koma chinthu kapena munthu amene chifanizirocho chimaonetsera ndiye chofunika kwambirie.

3. Chithunzi, chifanizo.
4. Anthu.
 - Malo
 - Zinthu zochitika.
 - Zinthu zakuthupi.
5. Yosefe.
6. Yesu Khristu.